

TINGATHE KUKHULUPIRIRA MWA MULUNGU

Nthawi ina Jim anafunsa munthu wosakhulupirira kuti kodi kuli Mulungu? Ngati anayamba waganiza mozama ngati kunjakuno kuli Mulungu kapena ai.

'Mwachuchuchu', munthuyu anati kwa Jim "zaka za m'mbuyomu pamene mwana wathu woyamba anabadwa; ndinatsala pang'ono kukhulupirira kuti Mulungu aliko; poona kanthu kakang'ono kangwi mu kama wake; tizala take tikugwedera ndi timaso take tikuphethira. kwa miyezi ingapo ndinali pafupi kusintha maganizo anga akuti kumwamba kulibe Mulungu" Izi zinamudabwitsa Jim.

"Pokaona kamwanako, ndinatsala pang'ono kukwanitsidwa kuti kuyenera kukhala Mulungu". Anapitiriza motero.

1. CHOPANGIDWA CHIRICHONSE CHIRI NDI OCHIPANGA WACHE



Kapangidwe ka thupi la munthu kayenera kukhala ndi mwiniwake wolipanga. Anthu otumbatumba ndi ofufuza amatiuza kuti ubongo umasunga ndi kukumbukira zinthu umapeleka mayankho ku mafunso, umaganiza, umayamikira zinthu zomwe zili zabwino ndiponso umalamulira minofu ndi zochitika zonse za mthupi la munthu.

Makina a kompyuta amagwira ntchito yonga iyi komabe zimatengera maganizo a munthu kupanga makina ngati amenewa.

Nzosadabwitsa kuti wolemba masalimo anafika ponena kuti thupi la munthu limanena momveka bwino komanso mofuula za mlengi woziwitsa:-

"Ndikuyamikani cifikwa kuti cipangidwe changa nchoopsa ndi chodabwitsa: Ntchito zanu nzodabwitsa; moyo wanga uchidziwa ichi bwino ndithu." - Masalimo 139:14.



Sitiyenera kupita kutali kuti tipeze ntchito za Mulungu Mmene ubongo wa munthu ndi ziwalo zina za thupi lake zinapangidwira zimalozera kunzeru zosafikirika za luso za ntchito ya Mulungu.

Palibe chopopera chiru chonse chopangidwa ndi munthu chingayerekezedwe ndi mtima wa munthu. Palibe mgwirizano wa mauthenga odzera mu makina a kompyuta womwe ungapose ngwirizano wa bongo ndi ziwalo zonse za thupi. Palibe ngwirizano wa mmene wailesi ya kanema igwirira ntchito yake womwe ungapose mmene munthu ayankhulira kumvera ndi kuona.

Palibe makina obweretsa mphepo yabwino kapena kutentha Munthawi yozizira omwe angapose ntchito ya mphuno ndi khungu.

Mmene thupi lamunthu liliri malukidwe ake ndikugwirizana kwake zimasyoneza kuti wina wake analipanga motero; ndipo wolipangayo ndiye Mulungu.

Thupi lamunthu ndi lathunthu zochitika za ziwalo zonse ndi zogwirizana mu ntchito zawo ndiponso zinapangidwa mosamalitsa. Mapapo ndi mtima; minofu ndi zotenga mauthenga kuchoka ndi kupita kuubongo; zonse ndi zogwirizana pa ntchito zofunika zosokonezekwa kuzimvetsetsa kwake; zomwe zifunikanso zipangizo zofanana nazo.

Mutatenga ndalama zachitsulo khumi ndikuika chizindikiro pa iri yonse ndi kuziika mthumba lanu ndikuzisakaniza mmenemo; ndipo nimuziturutsa, komanso nimuyamba kuzibwezeramo iriyonse payokhapayokha; kodi mwayi ulipo wotani kuti zibwezeredwemo mwandendende, kufanana ndi mmene zinaikidwira poyamba. Ai ndikwapatali kuti zitero.

Potsatira lamulo la masamu, mwina mwayi ulipo umodzi basi pa kuyesa kwa zikwi zikwi kuti zingaikidwe mundondomeko yake.

Ndiye inu onani mwayi wa mimba, ubongo, mtima, chiwindi, njira za magazi, impysyo, makutu, maso ndi mano zonse kukulira limodzi; kuyamba kugwirira ntchito limodzi; ndi nthawi imodzi. Kutheka kwa zonse ndi chinsinsi cha Mulungu.

Ndiye pamenepe, tingalilongosole bwanji momveka thupi la munthu ndi mapangidwe ake?

"Ndipo anati Mulungu, tipange munthu mchifanizo chathu monga mwa chikhaliidwe chathu: alamulire pa nsomba za m'nyanja, ndi pa mbalame za m'mlengalenga, ndi pa zonse zakukwawa pa dziko lapansi. Mulungu ndipo adalenga munthu m'chifanizo chake, m'chifanizo cha Mulungu adalenga iwo mwamuna ndi mkazi." - Genesis 1:26, 27.

Mwamuna ndi mkazi woyamba sanakhale mwatsoka ayi koma mwa chilinganizo. Bukhu Lopatulika likutsimikizira kuti Mulungu anawapanga iwo muchifanizo chake. Anataganizira natipanga kuti tikhaleko.

2. CHIRICHONSE CHOPANGIDWA CHIRI NDI WOCHIPANGA

Chotsimikizira kuti kuli Mulumgu sithupi la munthu lokha ayi. Zafalikira mpaka pa za kumwamba. Onani m'mene mlengalenga mumaonekera usiku. Mitambo yowundana pamwamba pa nyenyezi ndi njira zake zopangidwa ndi gulu la nyenyezi zikwi zikwi zowala ndi dzuwa lofanana ndi lathu lomwe tilidziwali.

Dzuwa lathu ndi maiko ake lizungulira ndi mbali imodzi miyanda miyanda ya nyenyezi zowala kwambiri zomwe zingaonedwe pansi pano ndi makina otchedwa "Telescope" amphanvu kwambiri, kapena "Hubble Telescope" Mumlengalenga.

Nzasadabwitsa kuti wolemba masalimo anafika ponena kuti, nyenyezi zimanena za ulemelero wa Mulungu.


"Zakumwamba zimalalikira ulemerero wa Mulungu; ndipo thambo lionetse ntchito ya manja ache." - Masalimo 19:1-3.

Nanga tingabwere ndi maganizo anji poona mapangidwe odabwitsa ndi kukula kwake kwa dziko lapansi?

"Pachiyambi Mulungu adalenga kumwamba ndi dziko lapansi." - Genesis 1:1.

"(Mulungu) ali woyamba wa zonse, ndipo zonse zigwirizana pamodzi mwa iye." - Akolose 1:17.

Zolengedwa zonse zichitira umboni Mulungu mwini wakuzipangayo. Mu mawu ena. "Pachiyambi Mulungu" tingawantanthaузire mosabvuta kuti tipezamo mayankho a zodabwitsa za m'moyo. Pali Mulungu amene analenga zonse.



Maganizo ambiri a akatswiri a zofufuza lero amakhulupiriranso kuti kuli Mulungu. Dr. Arthur Compton, yemwe anapeza mphotho pa zaukatswiri wake; ponenapo za vesi la m'bukhu lopatulikali anati;

Kwa ine ndimakhulupira kuti nzeru zodabwitsa zazikulu ndi zakuya zimabweretsa zinthu zomwe kunalibe, kukhalapo ndizomwezonso zinalenga munthu. Izi sizobvuta kwa ine kukhulupirira podziwa kuti paliponse pali cholengedwa pali Mlengi. Dziko lapangidwa mwa ndondomeko lichitira umboni ku coonadi cha mau oposa awa akuti, (PACHIYAMBI MULUNGU").

Bukhu lopatulika silikufufuza kuti lipeze zoona zake za Mulungu ayi, koma likunena za kukhalako kwake. Dr. Arthur Conklin, katswiri wodziwika pa zamoyo, analemba nthawi ina, kuti, "Maganizo oti pali mwayi woti moyo unachokera kwina kwake mwangozi angayerekezedwe ndi maganizo oti pali mwayinso woti pali buku lotanthauzira mawu losokonekera m'matanthauzo ake lomwe linabwera mwangozi pamene nyumba yosindikizira mabukhu inaphulika".

Tikudziwa kuti munthu sangapange kanthu popanda zipangizo zirizonse. Titha kumanga zinthu, kupeza zinthu zatsopano zomwe sizinawonedwepo, kulumikiza zinthu; koma sitinabweretsepo ngakhale kanthu kakang'ono popanda kugwirtsa ntchito zipangizo. Ine ngakhale kulenga chule kapena duwa laling'ono munthu sangathe.

Zinthu zomwe zitikhudza ife zimaneneranso kuti Mulungu anazipanga, anazirenga, nazipatsa umoyo wake. Yankho lenileni lokhulupirika pa chiyambi cha dziko lino lapansi, ndi anthu ake ndi - Mulungu.

3. MULUNGU AMABWERA M'CHIYANJANO NDI ANTHU

Mulungu yemwe anakhazikitsa nyenyezi m'mwamba, natenga dziko lapansi, amafuna kuyanjana ndi ife. Analu m'chiyanjano chomwecho ndi Mose: (Ndipo Yehova ananena ndi Mose... monga munthu alankhula ndi bwenzi lake" (Eksodo 33:11). Ndipo Mulungu akufuna kukhala m'chiyanjano ndi inu kuti akhale bwenzi lanu. Yesu anawalonjeza omutsatira ake: "Muli abwenzi anga inu" (Yohane 15:14).

Takhala tikulingalira tonse pa maganizo a za Mulungu, Pakuona munthu ndi waumulungu m'chibadwidwe. palibe nyama yomwe imanga guwa lopembedzerapo. Koma kuli konse mukapeza munthu (amuna ndi akazi) akupembedza. Mumtima mwa munthu ali yense muli chibadwidwe chakufuna kupembedza; kusonyeza kuzindikira kuti Mulungu aliko, ndi kufuna kukhala bwenzi lake.

Tikafunafuna motere ndi kumupeza Mulunguyo, sitikayikanso zakuti aliko ndi kumufuna kwathu.

Mu zaka za mu ma 1990, zikwi zikwi za anthu osakhulupira kuti kuli Mulungu m'dziko la Russia anasiya kusakhulupirira kwavo natembenukira kwa Mulungu.

Mphunzitsi wina wamkulu wa pa sukulu ina ya ukachenjede, St. Petersburg, ananena mau omwe anasonyeza anagwirizana ndi ganizo loti kunja kuno kuli Mulungu.

Iye anati "Ndafufuza tanthauzo la moyo mu ntchito yanga ya zofufuza, koma ndapeza zonse zosadalirika.. Anzanganso muntchitoyi sanapeze kanthu. Poyang'ana ukulu wa dziko lapansi ndi mmwamba ndi kuyerekeza ndi kuperewera kwa mzimu wanga; ndinamva china chake chosonyeza kuti payenera kukhala chinthu china cake chatanthauzo, ndipo nditalandira buku lopatulika ndikuwerenga, kuperewera kwanga kunakwanitsidwa tsopano m'moyo mwanga. Ndapeza kuti Bukhu lopatulika ndiye muli chilimbikitso cha moyo wanga. Ndamulandira Yesu kukhala mpulumutsi wanga ndipo ndapeza mtendere weni weni ndipo ndakhutitsidwa mu moyo wanga".

Mkhrisitu amakhulupirira mwa Mulungu chifukwa iyeyo wakumana naye ndikupeza kuti iyeyo amakwanirtsa zofuna za mtima wa munthu zenizeni. Mulungu, yemwe okhulupirira amupeza

mokondwera kuti aliko, amatipatsa ife maganizo atsopano, matanthauzo atsopano, zolina zatsopano ndi zisangalalo zatsopano.

Mulungu salonjeza moyo wopanda mavuto ndi zipsinjo ayi; koma alonjeza motitsimikizira kuti atsogolera ndi kutisungabe ife tikakhala naye m'chiyanjano. Miyanda miyanda ya akhirisitu idzachitira umboni kuti kuli bwino kusiya zonse ndi kukhala m'chiyanjano ndi Mulungu koposa kubwerera njira zakale zopanda Mulungu m'moyo.

Chodabwitsa chachikulu cha zonse ndi chakuti Mulungu wathu ndi Mlengi wathu amene amasunga ndi kuyang'anira dzikoli amafunanso kukhala m'chiyanjano ndi munthu aliyense, wamwamuna kaya wamkazi; mnyamata kapena mtsikana. Davide anakondwa ndi mawu awa pomwe analemba kuti:-

"Pakuona ine thambo la kumwamba lanu, ntchito ya zala zanu, mwezi ndi nyenyezi, zimene munazikhazika, munthu ndani kuti mumkumbukila?" - Masalimo 8:3, 4.



Mlengi wathu "amakumbukira" wina aliyense waife. Amakhala ndi chidwi ndi munthu aliyense payekhapayekha ngati kuti munthuyo alipo yekhayo basi yemwe anamulenga.

Choncho titha kukhulupirira mwa Mulungu:-

1. Chifukwa cha mphamu yake yodabwitsa yakulenga chirichonse cholengedwa.
2. Chifukwa cha kutifunafuna kwake kutipangitsa kusapeza bwino mpaka nafenso titamufunafuna ndi kumupeza, kuti tikapeze mpumulo mwa iye
3. Chifukwa chakuti pamene timufunafuna ndikumpeza lye Mulunguyo amatikwanirtsia mzosowa zanthu mosapereweza

4. KODI IYEYU NDI MULUNGU WA MTUNDU WANJI

Ndizoyenera kuti Mulungu mwini afuna kudziulula yekha kwa zolengedwa zake monga mmene bambo afunira kuti ana ake amudziwe. Ndipo mu buku lopatulika, Mulungu akutiuzza za iye mmene aliri ndi mmene aonekera.

Kodi Mulungu adagwiritsa ndondomeko yanji polenga amuna ndi akazi?

"Mulungu ndipo adalenga munthu m'chifanizo chake, m'chifanizo cha Mulungu adalenga ife; adalenga iwo mwamuna ndi nkazi." - Genesis 1:27.

Pokhala olengedwa m'chifanizo cha Mulungu, mwayi wathu wakuganizira, kumva, kukumbukira ndi chiyembekezo, kuona ndi kutanthauzira - zonse zichokera kwa lye.

Kodi khalidwe lenileni la Mulungu ndilo liti?

"Mulungu ndiye chikondi." - 1 Yohane 4:8.

Mulungu amadzilunzitsa ndi anthu achikondi, palibe chomwe anachita kapena adzachita choposa icho chosonyezera chikondi chake chodzipereka.

5. MMENE YESU AONETSERWA MMENE MULUNGU ALIRI

Mubukhu lopatulika, Mulungu ananena za iye yekha ngati atate.

"Kodi sitili naye atate mmodzi ife tonse? Sanatilenga kodi Mulungu mmodzi?" - Malaki 2:10.

Zifanizo zina za utate wake zomwe tiziona lero nzoyenera kuzisirira ndithu. Pali abambo ozunza ndi osasamala. Koma Mulungu sali choncho ayi. Iye ndiwosamala, ndiwokhudzidwa nafe. Iye ali ngati tate yemwe akucheza ndi ana ake nawasangalatsa powauza nthano za mbukhu lopatulika asanagone.

Atate wathu wokonda ankafuna kuchita mposera kudziulula yekha mu mawu ake oyera. Ankadziwa lye kuti munthu yemwe tikhala naye ali weniweni osati wongomumva kapena kumuwerenga mu buku ayi. Ndiye anadza ku dziko lino ngati munthu weniweni - munthu mwa Yesu.

"(Yesu) ali fanizo la Mulungu wosaonekayo." - Akolose 1:15.

Ndiye ngati mwaona Yesu, mwaona Mulungu. Anadza mooneka ngati ife - nakhala monga ife - kuti atiphunzitse mmene tiyenera kukhalira ndi kukhala okondwa; kuti tikathe ife kuona momwe aliri Mulungu. Yesu ndi Mulungu wopangidwa woonekayo. Iye anati, "Iye amene wandiona Ine waona Atate" (Yohane 14:9).

Pamene muwerenga mbiri ya Yesu mu mauthenga abwino anayi, omwe ndi mabukhu oyambirira anayi a chipangano chatsopano, mupeza maonekedwe oonetsa kuti Mulungu ali Atate wathu wakumwamba.

Asodzi aukali anasiya mauconde awo namutsata Yesu Khristu; ena anamuthamangira kuti akalandire madalitso. Atatha kusangalatsa wochimwitsitsa ndi kumuchepetsa uyo wodziyesa wolungama monyenga. Anachiza matenda ali wonse kuyambira ku khungu mpaka ku khate. Muntchito zake zonse, Yesu anaonetsa kuti Mulungu ndi chikondi ndipo wakhala ali chikondi chaulemerero, Yesu anafika pachimake poonetsa chikondi cheni cheni cha Mulungu pa mtanda.

"Pakuti Mulungu anakonda dziko lapansi kotero, kuti anapatsa mwana wake wobadwa yekha kuti yense okhulupirira iye asatayike koma akhale nawo moyo wosatha." - Yohane 3:16.

Yesu anafa osati kuti atipatse moyo wokondwa wa nthawi ino yokha ayi, komanso moyo wosatha. Kwa nthawi yaitali anthu akhala akuzizwa, kuyembekezera ndi kuganizira za Mulungu. Akaona chilengedwe chake padziko ndi kumwamba chiru chokongola. Koma pamtanda, Yesu anaphwanya zonsezi, nawapanga anthu kumuona Mulungu ndi chikondi chake chosatha maso ndi maso.

Mutha kumupeza Mulungu panopa pamene Yesu akumuvumbulutsa. Kupeza uku kukupangitsani kunena motsimikiza kuti "Atate, ndikukondani".



TITHA KUKHULUPIRIRA BUKHU LOPATULIKA

Oukira kapena kuti ogalukira otchuka omwe anamiza sitima ya azungu anakapezeka ali ndi azimayi a kwavo pa chisumbu cha 'Pitcairn' ku mwera kwa Pacific, okhaokha. Linali gulu la azungu asanu ndi anayi, amuna a chi Tahiti asanu ndi m'modzi, akazi a chi Tahiti khumi ndi msungwana wa zaka khumi ndi zisanu.

M'modzi wa a panyanjawa ankadziwa kutcheza mowa ndipo chifukwa cha izi uchidakwa udaononga pa chisumbupo. Kumakhala nkhanza zoopsa chifukwa amuna ndi akazi sankachedwa kumenyana ndipo adayamba kuphana. Patatha nthawi, m'modzi yekha wa anthuwo ndiye adapezeka ali ndi moyo. Koma munthuyo, Alexander Smith adapeza Bukhu lopatulika mu limodzi lamabokosi omwe anali musitimayo.



Anayamba kuliwerenga ndikuphunzitsa kwa ena zomwe anawerengazo. Moyo wake unapezeka wosinthika, ndiponso miyoyo ya anthu omwe anawaphunzitsa aja inasinthika. Anthu a pachisumbuwa anali olekanitsidwa ndi anthu ena onse a padziko mpaka pomwe opulumutsa a chi America anawapeza muchaka cha 1808. Gulu la anthuwa linapeza anthu apachisiwa akukhala mwa chipambano, kopanda mowa, ndende, kapena uchigawenga. Bukhu lopatulika linali litawasinta anthuwo kuwachotsa ku chitaiko chadziko lapansi kifika pa chidzalo cha momwe Mulungu afunira kuti anthu adzikhalira mdziko ndipo liri mpaka lero.

Kodi Mulungu akulankhulabe ndi anthu ake kupyolera mu masamba a m'bukhu lopatulika? Inde akuterodi. M'mene ndikulemba izi, ndikuona pa mayankho omwe tatumiziridwa kuchokera kwa ophunzira buku lopatulika pa sukulu yathu. Pansi pake waikapo mau akuti, "Ndiri m'ndende kudikira imfa chifukwa cha mlandu womwe ndidapalamula. Ndisadayambe maphunziro a buku lopatulikawa, ndinali wosohera; koma pano ndiri ndi chiyemekezo ndipo ndiri ndi chikondi chatsopano.

Bukhu lopatulika liri ndi mphamu yosinthira miyoyo ya anthu. Anthu amasinta kwambiri pamene awerenga Bukhu lopatulika.

1. M'MENE MMULUNGU AMAYANKHULIRA NDI IFE KUPYOLERA MU BUKHU LOPATULIKA

Atalenga anthu oyamba, Adamu ndi Hava; Mulungu amayankhula nawo maso ndi maso. Koma atachimwa, Mulungu nawayendera; banjali linachita chiyani? Linabisala

"Ndipo anamva mau a Yehova Mulungu ali n'kuyendayenda m'minda nthawi ya madzulo: Ndipo anabisala Adamu ndi mkazi wake pamaso pa Yehova Mulungu pakati pa mitengo ya m'munda." - Genesis 3:8.

Chimo linasokoneza kuyankhulana kwa maso ndi maso ndi Mulungu. Chimo litabwera padziko, Mulungu anayankhula bwanji kwa anthu ake?

"Pakuti Ambuye Yehova sadzachita kanthu osaulula chinsinsi chake kwa atumiki ake aneneri." - Amosi 3:7.




Mulungu sanatisiye ife mum'dima pa za moyo ndi tanthauzo lake. Kupylera mwa aneneri ake wawaitanira kulemba ndi kunenera za lye. Watiuulira ife mayankho a mafunso akulu m'moyo.

2. KODI ANALEMBA BUKHU LOPATULIKA NDANI?

Aneneri anapereka uthenga wa Mulungu polankhula ndi kulemba akadali ndi moyo. Pamene anafa, zolembera zawo zinakhala ziripobe. Maulauli awo anachitika ndi chitsogozo cha Mulungu, kupanga Bukhu lopatulika.

Kodi nanga zolemba zawozi ndizodalilika bwanji?

"Ndikudziwa ichi poyamba, kuti palibe chinenero chalembo chitanthauzidwa pachokha, pakuti kale lonse chinenero sichinadza ndi chifuniro cha munthu, koma anthu a Mulungu, ogwidwa ndi mzimu woyerana analankhula." - 2 Petro 1:20, 21.



Anthu olemba bukhu lopatulika adalemba zomwe anauziridwa ndi mzimu wa Mulungu, osati zofuna ndi zokhumba zawo ayi. Bukhuli ndi la mwini wake Mulungu.

Mubukhu lopatulika, Mulungu akutiu zamo za lye mwini ndikutiululira za cholinga chake pa munthu ndi mtundu wake. Likuonetsarano maganizo a Mulungu m'masiku akale, ndikutsegulira tsogolo, potiuza m'mene choipa chidzathetsedwere ndi m'mene mtendere udzabwerere pa dziko lapansi.

Kodi zonse ziri mu Bukhu lopatulika ndi uthenga wochokera kwa Mulungu?

"Lemba liri lonse adaliuzira Mulungu, ndipo lipindulitsa pa chiphunzitso, chitsutsano, chikonzero, chilangizo cha m'chilungamo: Kuti munthu wa Mulungu akhale woyenera, wokonzeka kuchita ntchito iri yonse yabwino." - 2 Timoteo 3:16, 17.

Bukhu lopatulika limakhudza kwambiri anthu chifukwa "zonse ziri m'menemo, ziri zouziridwa ndi Mulungu. Bukhu la Mulungu ndilouziridwa.

Aneneri analunzanitsa zomwe anaona ndi kumva ndi chilankhulidwe cha anthu, koma uthenga wao unachokera mwachindunji kwa Mulungu. Choncho, ngati mufuna kudziwa tanthauzo la moyo, werengani malembo opatulika. Kuwerengaku kudzakusinthani m'moyo wanu. Ndipo pamene muwerenga ndi pemphero, ndi pamenenso mtendere wamumtima uchulukira-chulukirabe mwa inu.

Mzimu woyerana omwewo unauzira aneneri kulemba Bukhu lopatulika, umapangitsa ziphunzitso zake, uthenga wake kukhala ndi mphambu yosinthira moyo wanu ngati mwaitana Mzimuyo kuti akhale nanu pamene muwerenga Bukhuli.

3. M'GWIRIZANO WA BUKHU LOPATULIKA

Bukhu lopatulika lapangidwa ndi mabukhu makumi asanu ndi limodzi, mphambu zisanu ndi limodzi (66). Mabukhu makumi atatu mphambu zisanu ndi zinayi (39) ndiwo a chipangano cha kale omwe anapangidwa mzaka za pakati pa 1450 BC ndi 400 BC. Mabukhu otsalawo makuni awiri mphambu zisanu ndi ziwiri (27) ndiwo a m'chipangano cha tsopano omwe anapangidwa mzaka za pakati pa AD 50 ndi AD 100.

Mneneri Mose ndiye adayamba ndi mabukhu oyambilira asanu a mu Baibulo, nthawi isanafike zaka za 1400 BC. Mtumwi Yohane analemba Bukhu lomaliza Chivumbulutso mzaka zapafupi-fupi AD 95. Mu

nthawi ya zaka chikwi ndi mazana asanu (1500) pakati pa nthawi ya kulemba bukhu loyamba ndi lomaliza la mu Baibulo, pafupi-fupi olemba ena ouziridwa makumi atatu mphambu zisanu ndi zitatu (38) anaperekapo maganizo awo. Ena a iwo anali ochita malonda, ena abusa aziweto asodzi, asilikali, madokotala, alaliki, mafumu, anthu antchito ndi machitidwe osiyana-siyana m'moyo uno.

Anthu onsewatu samachita ndi maganizo wofanana ayi. Koma choziwitsa cha zonse ndi ichi kuti: Pamene mabukhu onse makumi asanu ndi limodzi, mphambu zisanu ndi limodzi (66), ndi mitu yake chikwi zana limodzi makumi asanu ndi atatu mphambu zisanu ndi zinayi (1,189) kupanga mavesi zikwi makumi atatu ndi limodzzi makumi asanu ndi awiri mphambu zitatu (31,173) anabweretsedwa pamodzi kupezamo mgwirizano wa ngwiro wa mauthenga onse operekedwa m'menemo.



Kodi tiyerekeze kuti munthu wogogoda pa khomo la nyumba yanu, ndipo pamene mwamuza kuti alove, iye aika mwala wa maonekedwe osokonekera pa bwalo la chipinda chanu chochezera, nachoka osanena kanthu. Enanso alendo okwanira makumi anayi nabwera momutsatira kuchita chimodzi-modzi.

Pamene womaliza wapita, namuona modabwitsidwa kuti chifanizo chokongola chaimitsidwa pamaso panu. Ndipo namupeza kuti "okonza" zifanizo ambiri sanaonepo koma nabwera, monga anachitira, ali yense ndi mwala womwe wapanga kwayekha, wina kumwera kwa America, wina ku China, wina ku Russia, wina ku Africa, ndi mbali zina za dziko lapansi. Mukanakhala ndi maganizo anji poona kuti kulumikiza miyala yaoyo kwapanga chifanizo chokongola ngati chimenechi.

Mwina mukanaganiza kuti wina wake anatumizira aliyense muyeso weni-weni ndi maonekedwe a mwala umene ayenera kupanga.

Bukhu lopatulika lonse litibweretsera uthenga umodzi wogwirizana monga ngati chifanizo chija. M'modzi yekha ndiye anapanga maganizowa, ndiye Mulungu. Kugwirizana kwa malembo a mu Baibulo ndi umboni kwa munthu, kuti kupyolera mwa munthu, maganizo a Mulungu anauziridwa kuti alembedwe.

4. MUTHA KUKHULUPILIRA BUKHU LOPATULIKA


Kasungidwe ka Baibulo ndi kodabwitsa ndithu. Zolembedwa zoyambilira zinalembedwa pa manja, makina osindikiza mabukhu asanakhaleko. Alembi ankakopera zakalezo ndikumazigawira kwa anthu. Zikwi zikwi za zomwe anakopera kapena mbali zake zina zikupezekabe mpaka lero.

Zolembedwa za chi Hebre za chipangano chakale za mzaka za pakati pa 150 ndi 200 asanabadwe Yesu khristu zinapezeka pafupi ndi nyanja ya kufa (Dead Sea) mu chaka cha 1947. Ndizodabwitsa kuti zinthu zomwe zinakhala zaka zikwi ziwiri chilembedwere zili ndi uthenga wofanana ndi womwe uli mu chipangano chatsopano cha Baibulo lathu lero. Uwu ndi umboni wamphamvu wa m'mene Mau a Mulungu aliri mukudalirika kwake.



Poyambilira, atumwi analemba zambiri za m'chipangano chatsopano ngati makalata opita kwa Akhristu a mipingo yomwe inakhazikitsidwa Yesu atafa ndi kuuka. Pafupi-fupi makalata zikwi zinayi mazana asanu (4500) a mchipangano chatsopano kapena mbali zao zikupezeka zikuonetsedwa ku malo oonetsa zinthu zakale ndi malo owerengera mabukhu otchuka ku ulaya ndi America. Ena ndi akale kwambiri. Poyerekeza zimenezi ndi Baibulo lathu lero, tipeza kuti chipangano chatsopano chiri m'mene chinalembedwera palibe chomwe chasinthidwapo ayi.

Lero, kwapezeka kuti Bukhu lopatulika ndi zolembedwa zochokera mu Baibulo zimasulidwa mu ziyankhulo ndi m'manenedwe zoposera zikwi ziwiri, kudza makumi asanu ndi limodzi (2,060). Komanso ndi buku limene lagulitsidwa kwambiri pa dziko lonse lapansi. Pafupifupi kuposera mabaibulo zikwi zikwi zana ndi makumi asanu (150 million) ndi mbali zake amagulitsidwa chaka chiri chonse.



(2) Mbiri yachindunji ya Baibulo ndiyodabwitsa ndi yopatsa chidwi. Zofufuza zatsimikizira izi. Oona za mbiri apeza miyala ya dongo ndi zipilala za miyala zomwe zaonetsera maina, malo ndi zochitika zake zomwe zinalembedwa mu buku lopatulika lokha basi.

Mwachitsanzo, monga mwa Genesis 11:31, Abraham ndi banja lake "ndipo anaturuka pamodzi nao ku Uri wa ku Kaldayo kuti amuke (ku dziko la) kanani."

Chifukwa Baibulo lokha ndilo linena za Uri, ophunzira ambiri akhala akunena kuti mzinda umenewu sunayambe wakhalapo ayi. Ofufuza za mbiri yakale adapeza nsanja ya kachisi kumwera kwa Iraq yomwe anaifukula napezapo kuti inali ndi chonga ndowa pansi pake pomwe panalembedwa m'chinenedwe cha Igupto ndipo panali liu ili la Uri, kenaka kunapezeka chivumbulutso cha

Uri ngati mzinda wa chitukuko choyambilira. Ndipo Uri ndi chimodzi mwa za mbiri yakale zotsimikizira uchindunji wa Baibulo. Mzindawu ndi zochitika zake zidaiwalika, Baibulo lokha ndilo lidasunga zonsezi mpaka pamene ofufuza za mbiri ya zinthu anatsimikizira kukhalako kwake kwa mzindawu.

(3) Kukwaniritsa mu nthawi yake kwa maulosi a Bukhu lopatulika kumatisonyeza kuti tiyenera kulikhulupilira. Mau a m'Bukhu lopatulika ali ndi maulosi ambiri a zakutsogolo zomwe tikuziona ndi maso athu zikukwaniritsidwa. Timatha kufufuza mwakuya ena mwa maulosi opatsa chidwiwa, onena za maphunziro a mtsogolo.

5. TINGALIMVETSETSE BWANJI BUKHU LOPATULIKA?

Pofufuza za mau a Mulungu, kumbukirani mfundo izi:

(1) Werengani Baibulo ndi mtima wa pemphero. Ngati mutero, kumakhaladi kuonana maso ndi maso ndi Khristu pamene muwerenga mau ake (Yohane 16:13-14).

(2) Werengani Baibulo tsiku liri lonse. Uwu ndiwo mfungulo wa mphamvu m'moyo wathu, kukumana ndi maganizo a Mulungu (Aroma 1:16).

(3) Pamene muwerenga, liloreni Baibulo lomwelo litanthauzire inu. Mufunse: Kodi wolembayu akufuna kunena chiyan? Pomvetsetsa chimene ndime yolembedwayo ikunena, titha kugwiritsa mwa nzeru, tanthauzolo mu moyo wathu lero.

(4) Werengani mutu uli wonse wa mu Baibulo paokha. Yesu anagwiritsa ntchito njira imeneyi. Kutsimikizira kuti lye ndiye Mesiya.

"Ndipo anayamba Mose, ndi kwa aneneri onse, nawatanthauzira iwo m'malembo onse zinthu za lye yekha." - Luke 24:27.



Posonkhanitsa zonse zomwe Baibulo linena pa mutu uli wonse, timapeza kumvetsetsa kosakaikitsa.

(5) Werengani Baibulo kuti mulandire mphamvu yokhalira mwa Khristu. Mu Ahebri 4:12, akunena za mau a Mulungu kuti ali akuthwa konse-konse. Nzoposa malembo a pa pepala chabe; koma ali chida chamoyo m'dzanga lathu polimbana ndi mayesero ku chimo.

(6) Mvetsetsani pamene Mulungu alankhula nanu mu malembo ake. Ngati munthu afuna kumvetsetsa mau omwe awerenga mu Baibulo pa mutu wina uli wonse, ayenera akhale olola kutsatira zomwe akuphunzitsidwazo (Yohane 7:17) osati zomwe anthu ena akuganiza, kapena mipingo ina ikuphunzitsira ayi.

6. BUKHU LOPATULIKA LINGASIN THE MOYO WANU

"Potsegulira mau anu paunikira; kuzindikiritsa opusa." - Masalmo 119:130.

Kuwerenga Baibulo kumalimbikitsa "kumvetsetsa" kwanu ndikukupatsani inu mphamvu yogenjetsera zizolowezi zoipa ndi zoononga; ndikukupangani inu kukula mu thupi, m'maganizo, m'makhalidwe ndi muuzimu.

Bukhu lopatulika limayankhula ndi mtima. Limachita mbali yaikulu ku zochitika mwa munthu - kubadwa, chikondi, ukwati, kukhala makolo, ndi imfa. Limachiza mabala akuya mu moyo wamunthu, tchimo ndi zotsatira zake zodzetsa chisoni.



Mau a Mulungu si buku la mtundu umodzi wa anthu ayi, kapena msinkhu umodzi, kapena mbadwo umodzi, kapena dziko limodzi, kapena chikhalidwe chimodzi cha anthu ayi. Ngakhale linalemedewa ku m'mawa, likudanda lira amuna ndi akazi a kumadzulo. Lifikira m'nyumba za odzichepetsa ndi nyumba zikulu-zikulu za achuma. Ana akonda nthano zake zosangalatsa.

Ziphona za m'Baibulo zilimbikitsa achinyamata. Odwala, amasiye, ndi okalamba apezamo chitonthozo ndi chiyembekezo cha moyo wabwino.

Pakuti Mulungu amagwira ntchito yake kudzera mu Baibulo, ilo liri ndi mphamvu. Limaphwanya mitima youma, ndi zovuta zamoyo, kuifewetsa ndikuidzadza ndi chikondi.

Taona Baibulo ife likusandutsa wambanda ndi wosuta modetsa nkhawa kukhala mphunzitsi woona ndi woongoka. Ndipo taona Bukhu lomweli likumuchotsa munthu pa chingwe chomwe amafuna kudzipachikapo kuti afe ndikumupatsa chiyembekezo pa kuyambanso mwatsopano. Baibulo limadzutsa chikondi pakati pa adani. Limapangitsa onyada kudzichepetsa, ndi odzikonda kukhala ochita za chifundo. Baibulo limatilimbikitsa tikafooka, kutisangalatsa pamene takhumudwa, kutitonhoza m'chisoni; kutitsogolera pamene sitikumvetsetsa, komanso kutipulumutsa pamene tathodwa. Limationetsera m'mene tiyenera kukhalira molimba mtima ndi kufa opanda mantha.

Bukhu la Mulungu, Baibulo, litha kusintha moyo wanu! Mupeza zambiri za izi momveka bwino pamene muwerengabe mopitiliza zolemba izi za "chotsogolera kupeza."

Chifukwa chiyani Baibulo linalemedewa kwa ife? Yesu akuyankha:-

"Koma zalembedwa izi (choonadi cha Baibulo) kuti mukakhulupilire kuti Yesu ndiye Khristu Mwana wa Mulungu, ndi kuti pakukhulupilira mukhale nawo moyo m'dzina lake." - Yohane 20:31.

Chifukwa chachikulu choti tikhale odziwitsitsa bwino mau opatulikawa ndi chakuti, muli zithunzi-thunzi za kwa ife za m'mene Yesu Khristu atitsimikizira ife za moyo wosatha. Poona Khristu Kupyolera mu Baibulo,

tinasinthika ndikukhala pafupifupi monga lye. Tsono bwanji osayamba tsono kufufuza ndi kupeza mphamvu za m'mau ake omwe angakupangeni kufanana ndi Yesu?

KODI MOYO WANGA NGOFUNIKA PAMASO PA MULUNGU



Nthawi zina dziko limaoneka labwino ngati Paradizo. Ukadzuka m'mawa, kupuma kupyolera pa zenera mmene duwa likualira mosangalatsa loonekera mmitengo, tsamba ndi tsamba la mtengo. Nthawi zina, zimapangitsa moyo kuoneka wofunika ndi wabwino: Nkhope ya bwenzi lokondeka amene akutsazikana nawe, tinyimbo tongodutsa tomveka mogwirizana ndi nthawi yace, komanso chikoka chosayembekezeza cha mwana wang'ono.

Koma nthawi zina, dziko limaoneka ngati malo atsoka. Ukadzuka mmawa nuwerenga nyuzipepa ndi mitu yake yonena za anthu oipsa anzao ataombera malo kupangitsa anthu kulumala; kukhala akhungu ndi ana omwe; komanso wakupha wina akupha munthu wake wachikhumi; komanso kwina njala ndi kusefukira kwa madzi kapena nkhondo ndi chivomerezi zitasautsa. Izzi ndi nthawi zimene chirichonse chimakhala chopanda pake, palibe chimaoneka chabwino.

Nanga zonzezi zitanthauzanji? Tingapezepo zinthu zenizeni mu dziko lodabwitsali ndi loopsali? Kodi tiriko chifukwa chiyani? Kodi moyo wanga uli wofunika kwa Mulungu kapena ndangokhala kanthu kena kake kakang'ono mu chimakina chachikulu kwambiri moti sindingaonekere?

1. MULUNGU ANALENGA DZIKO LANGWIRO



Mulungu ndi Mlengi; katswiri wolikonza ndi kuliona dziko m'mene lingakkhalire asanalipange kuona kuyambira ku nyenyezi yaikulu mpaka ku phiko la gulugufe.

"Zakumwamba zinalengedwa ndi mau a Yehova; ndipo ndi mpweya wa m'kamwa mwace khamu lao lonse.... Pakuti ananena, ndipo chinachitidwa; Analamulira, ndipo chinakhazikika." - Masalimo 33:6-9.

Mulungu amangolankhula kokha ndipo zinthu zonse zinamumvera m'chifuniro cace.

2. MASIKU ASANU NDI LIMODZI KUPANGA DZIKO LATHU

"Chifukwa masiku asanu ndi limodzi Yehova adamaliza zakumwamba ndi zapansi, ndi nyanja, ndi zinthu zonse ziri m'menemo, napumula tsiku lacisanu ndi chiwiri, chifukwa chache Yehova anadalitsa tsiku la Sabata kuti likhale lopatulika." - Eksodo 20:11.

Mulungu wamphamvu zonse ndi wamuyayaakanatha kulilenga dziko lonse mukamphindi "munthawi yakupuma kamodzi kwa lye" Koma lye anasankha kuigwira ntchitoyi masiku asanu ndi limodzi, mphindi

zisanu ndi limodzi kapena kucheperapo zinalinso zokwanira kwa lye. Mutu woyambirira mu Bukhu lopatulika, Genesis 1, likulongosola zomwe Mulungu analenga pa tsiku lirilonse la pamulungu.

Kodi chomalizira chofunika ndi chiti chomwe iye adalenga tsiku lachisanu ndi chimodzi?

"MULUNGU NDIPO ADALENGA MUNTHU M'CHIFANIZO CHAKE M'CHIFANIZO CHA MULUNGU ADAMLENGA IYE, ADALENGA IWO MWAMUNA NDI MKAZI." - Genesis 1:27.



Mulungu adaganiza zolenga munthu wofanana ndi lye yemwe akadatha kuganiza, kumva ndi kukonda, Munthu aliyense wapangidwa "m'chifanizo" cha Mulungu.

Pofika tsiku lachisanu ndi chimodzi, dziko linali litadzala ndi zomera ndi nyama, ndipo Mulungu anaonetsera cholengedwa chake chofunikira monga mwa Genesis 2:7, Mulungu wamphamu zonse adampanga Adamu ndi thupi lake kuchokera kudongo la panthaka. Ndipo pamene lye anauziramo "mpweya wa moyo" mu mfuno zake, munthuyu anakhala "wamoyo" - kutanthauza kuti anasandulika kukhala wamoyo. Mulungu anapanga munthu woyambayo Adamu m'chifanizo chake; Adamu, kutanthauza 'Mwamuna' ndi mkazi woyamba Hava, kutanthauza "Umoyo" (2:20; 3:20). Mlengi wokonda anaona kufunika kwa kukhala ndi wohandizana naye pa umunthu.

Chopangidwa mwatsopano ndi dzanja la Mulungu, Adamu ndi Hava, onse anaonetsadi chifanizo cha Mulungu. Mulungu akanatha kuwapanga iwo ngati ma roboti kuti azingowayendetsa m'munda wa Edeni mmene lye afunira ndi kuwauza kukweza mau awo motamanda lye. Koma Mulungu anafuna zambiri; Chiyanjano chenicheni. Maroboti kapena zidole za magetsi zitha kumwetulira, kuyankhula, ngakhale kutsuka mbale ngati mwawalamula; koma sizingathe kukonda.

Mulungu anatilenga m'chifanizo chake, ndi ufulu wonse wakuganiza ndi kusankha, kukumbukira, kumvetsetsa ndi kukonda mwatokha. Adamu ndi Hava anali ana a Mulungu, ndi ofunikira ndi okondedwa ndi iye.



MULUNGU (SABATA) WAKULENGA

Tsiku loyamba; Kuwala, ndondomeko ya usana ndi usiku.

Tsiku lachiwiri; Mlengalenga wa dziko lapansi.

Tsiku lachitatu; Dziko louma ndi zomera.

Tsiku lachinayi; Dzuwa ndi mwezi zinaoneka.

Tsiku lachisanu; Mbalame ndi nsomba.

Tsiku lachisanu ndi chimodzi; Nyama zakumtunda ndi Munthu.

Tsiku lachisanu ndi chiwiri; Sabata.

3. CHOIPA CHIDZA KU DZIKO LANGWIRO

Adamu ndi Hava anali ndi chirichonse chowapanga iwo kukhala okondwa. Anakondwa ndi kusangalatsidwa ndi thanzi lawo lathupi ndi maganizo, kukhala m'munda wokongola, nyumba ya dziko lopanda banga (Genesis 2:8; 1:28-31). Mulungu anawalonjeza iwo ana ndi mphamvu ya maganizo a kulenga, ndi kupeza chikwaniritso mu ntchito za manja awo (Genesis 1:28; 2:15). Anaonana naye

Mulungu maso ndi maso; popanda kalikonse kobweretsa chidandaulo, mantha, matenda, kuwasokoneza mu masiku awo abwinowo.

Nanga dziko linasinthika bwanji mwachangu kukhala malo a mazunzo ndi matsoka? Mutu wachiwiri ndi wachitatu wa bukhu la Genesis ukunena nthano yonse ya m'mene chimo linalowera mu dziko lapansi. Werengani panokha munthawi yanu. Koma pano tinena mwa chidule za nthanoyi.

Nthawi imene Mulungu anatha kupanga dziko langwi, mdierekezi anabwera m'munda wa Edeni kudzamuyesa Adamu ndi Hava kuti asamvere Mulungu Mlengi wawo. Koma Mulungu anachevertska ukulu wa yeso la mdierekezili ku mtengo umodzi wa mmundamo, "Mtengo wakudziwitsa zabwino ndi zoipa" Ndipo lye anawachenjeza awiriwo kuti asaukhudze ndipo asadye zipatso zake; apo ayi adzafa akadzadya.



Koma tsiku lina Hava ankayendayenda mouzungulira mtengo woletsedwawu. Pomwepo Satana anapezerapo mwayi wogwira ntchito yake. Anaonetsa kwa Hava kuti Mulungu wanama kwa iwo ndipo kuti akadzadya za mumtengowu adzakhala odziwa zabwino ndi zoipa, nakhala ndi nzeru ngati za Mulunguyo. Mwatsoka Hava ndi Adamu, omwe panthawiyi ankadziwa zabwino zokha zokha, anamulola Satana kuwanyenga, ndipo anadyadi zipatso za mumtengowu woletsedwawo - kuphwanya ubale wokhulupilirana ndi kumvera, Mulungu.

Mulungu anawakonzetsera Adamu ndi Hava "kulamulira" pa dziko lonse lapansi ngati adindo a zolengedwa zonse za Mulungu ndi ntchito yake (Genesis 1:26). Koma chifukwa iwo anaphwanya chikhulupiliro chawo ndi Mulungu, nasankha Satana ngati mtsogoleri wawo watsopano, iwo awiriwa anataya ulamuliro wawo. Lero Mdierkezi walitenga dziko lapansi ngati lake ndipo akuyesetsa kuwaika anthu mu ukapolo.

Nthawi zambiri timapezeka tiri odzikonda, ankhanza, ngakhale pamene sitifuna kukhala otero. Nanga ndichifukwa chiyani? Ndichifukwa chakuti, mdani wosaonekayo, Satana akugwira ntchito yake mwa anthu kuti alephere m'chikhaliidwe.

Pamene muwerenga mutu wachitatu wa bukhu la Genesis, mupeza kuti chimo linapangitsa Adamu ndi Hava kubisala pamaso pa Mulungu chifukwa cha mantha. Chimo linakhudza chilengedwe chonse. Mungalipeze muzomera ndi maluwa ake, kubereka kwa ana kunasanduka chinthu chowawa. Matenda adayamba kugwa nthawi ndi nthawi. Dumbo, chikhaliidwe cha unyama, kaduka zinakulirabe pakati pa mtundu wa anthu, ndipo zinawapangitsa kuoneka ozunzika. Choopsa cha zonse chomwe chinadza ndi utchimo ndicho imfa!

4. KODI MDIYEREKEZI AMENEYU NDI NDANI KUTI MPAKA AONONGE DZIKO LATHU LAPANSI NDI TCHIMO?

"Iyeu anali wambanda kuyambira pachiyambi,... pakuti mwa iye mulibe choonadi. Pamene alankhula bodza, alankhula za mwini wake; pakuti ali wabodza, ndi ATATE WACHE WA BODZA." - Yohane 8:44.

Malinga ndikufotokoza kwa Yesu, Mdierkezi ndiye chiyambitso cha tchimo mdziko lapansi, 'tate' wa tchimo mongatu kupha ndi bodza.

Thomas Carlyle, woganiza mwakuya pachinenero cha chingerezi anamtenga Ralph Waldo Emerson tsiku lina ndikuyenda naye mu misewu yoipitsitsa ya kummawa kwa mzinda wa London. Mmene amayenda, amayang'anitsitsa mwakachetechete zoipa ndi zambanda zonse zomwe zimachitika mowazungulira; pamapeto pake Carlyle anafunsa "ukukhulupilira mwa Satana mdiyerekezi tsopano"?

5. KODI MULUNGU ADAMULENGA MDIERKEZI?

Ayi! Mulungu wabwinoakanatha kulenga mdierekezi komabe Baibulo lopatulika likunena kuti Mdierekezi ndi angelo ake adawanyengawo, anataya malo awo kumwamba nabwera padziko lathuli lapansi

**"ndipo munali NKHONDO M'MWAMBA. Mikayeli ndi angelo
ache akuchita nkondo ndi chinjoka; CHINJOKANSO NDI
ANGELO AKE chinachita nkondo; ndipo sichinalakika, ndipo
SANAPEZEKANSO MALO AO M'MWAMBA. Ndipo
chinaponyedwa pansi chinjoka chachikuru, njoka yokalambayo,
iye wochedwa mdierekezi ndi satana, wonyenga wa dziko
lonse, chinaponyedwa pansi kudziko, ndi angelo ake
anaponyedwa naye pamodzi." - Chivumbulutso 12:7-9.**



Nanga Mdierenkezi adapezekako bwanji kumwamba moyambirira?

**"Unali KERUBI WODZODZEDWA WAKUPHIMBA, ndipo ndinakuika unali pa phiri lopatulika la
Mulungu... UNALI WANGWIRO M'NJIRA ZAKO CHILENGEDWERE IWE MPAKA CHINAPEZEKA
MWA IWE CHOSALUNGAMA." - Ezekiel: 28:14, 15.**

Mulungu sanalenge mdierenkezi ayi, koma adalenga Lusifala, m'ngelo wangwiyo, m'modzi waotsogolera angelo kumwamba, oima pafupi ndi mpando wa Mulungu. Koma tsono anachimwa - "chosalungama chinapezeka mwa iye." Woponyedwa pochotsedwa kumwamba, naonekera kwa Adamu ndi Hava ngati bwenzi, anasandulika m'dani woopsetsetsa wa munthu.

6. CHIFUKWA NINJI LUSIFALA, M'NGELO WANGWIRO ADACHIMWA?

**"WAGWADI KUCHOKERA KUMWAMBA, iwe nthanda, mwana wa m'banda kucha!
WAGWETSEDWA PANSI, IWE WOLEFULA ... ndipo iwe unati mumtima mwako 'ndidzakwera
kumwamba, ndidzakweza mpando wanga wa chifumu pamwamba pa nyenyezi za Mulungu;
NDIDZAFANANA NDIWAM'MWAMBAMWAMBA." - Yesaya 14:12-14.**

Munthu yemwe anasandulika mdierenkezi adali wotchedwa Lusifala pachiyambi, kutanthauza "nyenyezi ya tsiku" kapena "uyo wowala." Mumtima mwa m'ngeloyu uchabe ndi zikhumbo za moyo zinalowa m'malo mwa kudzipeleka kwake kwa Mulungu. Mbewu ya kudzikusa inakula mwa iye nibala zipatso zofuna kutenga malo a Mulungu. Lusifala anayesetsa ndi mphamvu zake zonse ponyengelera ena a kumwambako. Nzosavuta kumuganizira Satana akutsutsana ndi Mulungu pankhani yoti Mulunguyo wawabisira zina zomwe anayenera kuzidziwano, komanso kuti malamulo ake ndi okhwima ndipo iye ndi Mulungu wosasamala. Anamutsutsa uyo amene khalidwe lake liri kutanthauzira chikondi.

Kodi mkangano wa kumwamba unatha bwanji? "unadzikuza mtima chifukwa cha kukongola kwako,... ndakugwetsa pansi."

Kunyada kusanduliza mkulu wa angelo kuhala Satana Mdierenkezi, ndipo pofuna kuchinjiriza ufulu ndi mgwirizano wa kumwamba, iye satanayo ndi limodzi la magawo atatu la angelo linayenera kuchotsedwa (Chivumbulutso 12:4, 7-9).



7. KODI MWINI WAKE WA TCHIMO NDANI?

Kodi bwanji Mulungu sanalenge anthu oti sangachimwe? Akanatero, sikunakhala vuto la choipa chiru chonse m'dziko lathu. Koma Mulungu amafuna anthu amene angakhale mchiyanjano chomvetsetsa. Choncho "Iye (Mulungu) analenga munthu mchifanizo chake" (Genesis 1:27). Izi zikutanthauza kuti tiri ndi ufulu ndikudziyankhira pa machitidwe athu onse. Titha kusankha kumkonda Mulungu kapena ayi.

Mulungu anapereka kwa angelo ndi anthu a mbadwo uli wonse mzimu ndi mphamvu zakupanga okha chisankho.

"Mudzisankhire lero amene mudzamtumikira." - Yoswa 24:15.



Mulungu akuwabetchera anthu ake omwe adawalenga kusankha kuchita bwino chifukwa choona kuti "njira ya Mulungu ndi yabwino koposa," ndikusankha kuchoka ku choipa chifukwa maganizo awo akumvetsa zotsatira zake zoopsa zachoipacho. Anthu okhawo otha kuganiza ndi kusankha angathe kupeza chikondi chenicheni. Mulungu amafunitsitsa kulenga anthu omwe akanatha kuyamikira ndi kumvetsa khalidwe la Mulungu, namlandira lye mchikondi nakhalala ndi chikondi kwa ena. Mulungu amafuna kugawana nawo chikondi chake mpaka kuti anali olola koposa kulenga angelo ndi anthu a mphamvu zakusankha, chomwenso chinali chinthuschoopseza mpando wake. Ankadziwa kuti nzotheka kuti tsiku lina, chimodzi cha zolengedwa zake chitha kusankha kusamvera. Satana anali woyambilira kupanga chisankho choterechi padziko lonse. Tsoka la tchimo linayamba ndi iye (Yohane 8:44; 3:8).

8. MTANDA UNAPANGITSA TCHIMO KUKHALA LOTHEKA KULIONONGA

Chifukwa chiyani Mulungu sanaononge Lusifala tchimo lake lisanafalikire ku dziko lonse? Lusifala anaonetsa kuti ulamuliro wa Mulungu unali wopanda chilungamo. Ananena mabodza okhudza Mulungu.

Mulungu akanati amuononge iye nthawi yomweyo, angelo ambiri bwenzi akumupembedza ndi mantha osatinso ndi chikondi ayi. Ichi chikanapha cholinga cha Mulungu polenga munthu; anthu amene anali ndi mwayi wakusankha pachiyambi.

Kodi aliyense akanadziwa bwanji kuti njira yamoyo ndiyo inali yabwino koposa? Mulungu anapatsa Satana kuti aonetse njira inayo. Ndicho chifukwa chake anapatsidwa mwayi woyesa Adamu ndi Hava.

Dziko lino lakhala poyeserapo khalidwe la Satana ndipo ufumu wake ufananizidwa motsutsana ndi makhalidwe a Mulungu ndi ufumu wake. Ndani yemwe ali wolondola? Ndani amene tingamukhulupiliredi?

Lusifala analitu wonyengadi mpaka kuti patenga nthawi yaitali kuti anthu a dziko lapansi adziwe m'mene njira iliri yoononga. Koma pang'ono ndi pang'ono munthu aliyense adzaona kuti "mphotho yake ya uchimo ndi imfa ndi kuti "mphatso yaulele yaulemelero ya Mulungu ndi moyo wosatha mwa Yesu Khristu Ambuye wathu" (Aroma 6:23).

Munthu aliyense m'dziko adzabvomereza kuti **"Ntchito zanu ndizazikulu ndi zoziwitsa, Ambuye Mulungu wamphamvu yonse, njira zanu nzolungama ndi zonna, mfumu inu ya nthawi zosatha... chifukwa mitundu yonse idzadza ndizolambira pamaso panu, popeza zolungama zanu zidzaonetsedwa."** - Chivumbulutso 15:3, 4.

Aliyense atatha kuona kuopsa kwa chimo ndi chionongeko chobwera ndi ziphunzitso za Satana, Mulungu adzatha kuononga Satana ndi tchimo. Iye adzayeneranso kuononga iwo amene asankha moumilira kuchita tchimo ndi kutsatira mdierekezi.

Mulungu ali wa nkhwawa kuthetsa vuto la tchimo ndi kuvutika ngati timulola lye kuti atero. Koma lye akudikira mpaka pamene akachite izi



momaliziratu, mpakanso pamene angathe kusungabe ufulu wathu wa maganizo nthawi yomweyonso kuthetsa choipa kuti chisadzaonekenso.

Mulungu walonjeza kuthetsa tchimo kwa tuyaya poyeretsa kumwamba ndi pansi ndi moto. "Posunga lonjezo lakeli," titha kuona "kutsogolo kuyang'anira m'mwamba mwatsopano ndi dziko lapansi latsopano, kwoa kwa olungama" (2 Petro 3:10, 13). Tchimo silidzaipsanso dziko lapansi. Zotsatira zoopsa za chimo zdizaonekeraya, kuonetsera kuti kusamvera cholinga cha Mulungu kudzasonyeza kunyansa kwa tuyaya. Ndani apangtsa chionongeko chomaliza cha mdierekezi ndi tchimo?

"Popeza tsono ana ndiwo a mwazi ndi nyama, Iyenso (Khristu) momwemonso adalawa nawo makhalidwe omwewo kuti mwa imfa akamuononge iye amene anali nayo mphamvu ya imfa, ndiye m'dierekezi, nakamasule iwo onse amene, chifukwa chakuopa imfa, m'moyo wawo wonse adamangidwa ukapolo." - Ahebri 2:14, 15.

Pamtanda, Angelo ndi maiko osagwawo anamuona satana m'mene analiri, wonyenga, wabodza, wakupha . Apa anaonetsa khalidwe lake lenileni powamemeza anthu amuna kupha mwana wa Mulungu wosalakwa.



Anthu onse okhala mdziko lapansi anaona m'mene tchimo liriri lopanda tanthauzo ndi lankhanza. Mtanda unavumbulutsa zolina za satana ndi onse opitiriza mu uchimo, onse adzavomereza kuti Mulungu ndi wa chilungamo.

Imfa ya Yesu pamtanda inaonetsera poyerza zolina zenizeni za satana pamaso pa anthu onse olengedwa (Yohane 12:31, 32).

Mtandanso ukutionetsera m'mene Khristu aliri Mpulumutsi wa dziko. Pa Gologota, mphamvu ya chikondi cha Mulungu inaonekeraka motsutsana ndithu ndi chikondi cha pa mphamvu. Mtanda unaonetseratu mopanda kukaika kuti ndi chikondi cha kudzipereka nsembe chomwe chimamulimbikitsa Mulungu pa kuthana naye satana, tchimo, ndi amuna ndi akazi ochita tchimo.

Pamtanda, paja chionetsero cha chikondi cha Mulungu mwa Khristu chinagonjetsadi mdierekezi. Nkhondo inali pakati pa kupeza yemwe angalamulire dziko, Khristu kapena satana. Ndiponso mtandawo unaweruza kwa tuyaya pa nkhondoyi ayenera kukhala Khristu basi mwa zonse.

Kodi mwapeza ubale ndi Mpulumutsi yemwe anafa kuululira inu chikondi chake chosasintha? Mukumva bwanji za lye amene anabwera kudziko lapansi ngati munthu nafa m'malo mwanu kukupulumutsani ku zotsatira za tchimo? Mungaweramitse nkhope yanu panopa ndi kumuthokoza Yesu, ndikumupempa kuti adze kutenga moyo wanu?

CHIKONZERO CHA MOYO WANU

Mlaliki wina atatha kualikira pa mutu wotchedwa "CHIFUKWA CHOMWE NDIKHULUPIRIRA MWA YESU", munthu wina wovala mooneka bwino, wamwamuna anamuyendera wolalikirayu kukamuchezera mukuwerenga ndi kuphunzira kwake, ndipo anapereka ndemanga yakuti, "Uthenga wanu usiku uja unali wopatsa chidwi, koma zonse zomwe mumanena zimachokera mu baibulo lanu, zokhuza Yesu khirisitu, Ndiuzeni ine ngati Yesu anadzakhaladi mdziko lino lapansi? Nanga chifukwa chiyani mbiri iriyonse siyinena za lye?"

"Funso labwino limenelo," Anatero wolalikirayu yemwe anatembenuka natenga mabukhu angapo, nati, "Kunena, zoona mbiri ikunenapo za Yesu Khristu".

M'nyamatayu anayankhango nati, "Izi ndikufuna nditaziona ndekha".

(Chabwino, tengi iyi yomwe iri kalata ya panambala makumi asanu ndi anayi mphambu zisanu ndi ziwiri (97) ya mubukhu la chachikhumi la Pliny wang'ono, woyambirira wachiroma ku Bithynia, dela lina la ku Asia Minor. Pliny analembera kwa mfumu wa Roma, Trajan, kumuza za zomwe zichitike m'derali: Onani, apa akufunsa nzeru za mmene angachitire ndi kagulu katsopano, ka a khristu akunena za mmene kagulu kameneka kakuchulukirira mofulumira ndi momwe akuyimbira nyimbo zao mwanthenthemya zophunzitsidwa ndi atsogoleri awo. Kalatayi ikuonetsa mbiri yonse ya umboni wa mbiri ya munthu, Khristu ndi kulalikira kwa chikhulupiro chake mnthawi ya masiku atumwi ake".



EMPEROR
NERO

Modabwa m'nyamatayu anati, "ndiuzenibe Zambiri!" Pamene mbusayu amaloza ndi chala chake mizere ya mau yomwe amawerenga m'bukhu linanso, anaonjezera kunena yomwe amawerenga m'bukhu linanso, anaonjezera kunena kuti; " Wolemba za mbiri yakale winanso, mogwirizana ndi Pihiny, anali Tacitus, mtimabukhu take ting'onuting'ono, (Bukhu la chikhumi ndi chisanu, (15), mutu wa makumi anayi mphambu zinayi (44) akunena za udani wa mfumu Nero womwe anali nawo pa akhristu omwe adaphetsa akhristu nthawi yomwe Roma anadya moto. Tacitus kuti liwu loti "mkhristu" likuchokera ku dzina la "khristu". Akunenaponso kuti Yesu Khristu, yemwe adayambitsa chipembedzo cha chikhristu, anaphedwa ndi mfumu Pilato, wolamulira woweruza wa mu Yudeya, munthawi ya mfumu Pilato, wolamulira woweruza wa mu Yudeya, munthawi ya mfumu Tiberius. Zonsezitu Zomwe Tasita akutipatsa m'bukhuli zikugwirizana ndendende ndi zonse zochitika , maina ndi malo omwe apatsidwa mu Baibulo".

"Abusa, ndinali ndisanamvepo kuti zinthu ngati zimenezi zikupezeza mu mbiri yakale ya dziko lapansi!" Mlendoyu adafuala.

Mbusayu adaptiriza nati, "ndikufuna uwone kuti pafupifupi mu AD 180, Celsus analemba bukhu lotsutsa akhrisitu, kuonetsera kuti chikhristu munthawiyo chinali ngati chokakamiza kuchitsata". "Ngati ukukayikabe, kumbukira kuti mabukhu amauthenga abwino anayi aja a m'chipangano chatsopano ali ndi mbiri yakale ngati bukhu lina liri lonse la mbiri yakale".

Pamene mnyamatayu anazindikira kuti bukhu lopatulika ndi mbali zake komanso mabukhu wamba akugwirizana kuti Yesu anakhalapo monga munthu pa dziko lapansi, anapita wokhutitsidwa kuti Yesu Khristu alipodi weniweni, woonetsedwa mu mbiri yakale.

1. KHRISTU ANAYAMBA KUKHALAKO KUYAMBIRA KALE LOSAONEKALO

Yesu sanangokhala kokha munthu wabwino ayi, analinso Mulungu. Kodi Yesu adapanga chiyani yekha chokhudzana ndi Umulungu?

"Mukadazindikira Ine mukadadziwa Atate wanganso, kuyambira tsopano mumzindikira lye, ndipo mwamuna lye,... lye amene wandiona Ine waona Atate." - Yohane 14:7-9.

"Mulungu ndi ndani? nanga amaoneka bwanji?" Yang'anani kwa Yesu basi, yemwe ananena,

"Ine ndi Atate ndife amodzi." - Yohane 10:30.

Mulungu Atate ndi, Mulungu Mwana, akhala aliko limodzi kuyambira kalekale (Aheberi 1:8). Palibe nthawi yomwe Yesu anakhala yekha wopanda Atate. Mulungu Atate amachita mwa chikondi ndi chisamaliro chimodzimodzi monga chomwe Yesu anaonetsera mu moyo wake wonse pa dziko lapansi.



2. KHRISTU, MTIMA WA MBIRI YAKALE NDI ULOSI

Pakuti mbiri ya moyo wa Khristu imakwaniritsa ulosi, mbiri yakeyinso inalembedwa lye asanabadwe. Ulosi wa mu chipangano chakale umaonetseratu ndondomeko yonse ya moyo, imfa ndi kuuka kwa Yesu. Chipangano chatsopano ndiye moyo wakewo mokwaniritsa zomwe zinaloseredwazo.



Aneneri a chipangano chakale omwe adakhalako zaka pafupifupi kuyambira mazana asanu mpaka chikwi ndi mazana asanu Yesu Khristu asanabadwe, umaonetseratu molosera za moyo wonse wa Mesiya. Ndipo pachiyambi penipeni pa utumiki wa Yesu Khristu pa dziko lapansi, pamene anthu amafananitsa moyo wake ndi ulosi womwe udalipo wa lye, kodi adafika pa mfundo yomaliza yamtundu wanji?

"Iye amene Mose analembera za lye m 'chilamulo, ndi aneneri, tampeza, ndiye Yesu mwana wa Yosefe wa ku Nazarete." - Yohane 1:45.

Mpulumutsi wathu anaonetsa momwe lye aliri ndi ntchito yake kupiyolera mu ulosi wokwaniritsidwawo.

"Ndipo anayamba ndi Mose, ndi kwa aneneri onse, nawatanthauzira iwo m 'malembo onse (chipangano chakale) zinthu za lye yekha". - Luke 24:25-27.

3. MOYO WA KRISTU, KUKWANIRITSA ULOSI

Tiyeni tiwone angapo a maulosiwa momwe aliri mu chipangano chakale, ndi mmene akwaniritsidwira mu chipangano chatsopano.

MALO AKE OBADWIRA

Ulosi wa m 'chipangano chakale:

"Koma iwe, BETELEHEMU Efrata, ndiwe wamng'ono kuti ukhale mwa zikwi za Yuda. Mwa iwe mudzanditrukira wina wakudzakhala woweruza m'Israyeli; maturukiro ake ndiwo a kale lomwe, kuyambira nthawi yosayamba." - Mika 5:2.

Kukwaniritsidwa kwa ulosiwu m'chipangano chatsopano:

Kukwaniritsidwa kwa ulosiwu m'Betelehemu wa Yudeya." - Mateyu 2:1.

KUBADWA KWAKE MWA NAMWALI

Ulosi wa m'chipangano chakale: "**Taonani Namwali adzaima, nadzabala mwana wa mwamuna, nadzamucha dzina lake Imaneli? (Mulungu Nafe).**" - Yesaya 7:14.

Kukwanirtsidwa kwa ulosiu m'chipangano chatsopano:

"Yosefe, Mwana wa Davide, usaope kudzitengera wekha Mariya mkazi wako; pakuti ICHO CHOLANDIRIDWA MWA IYE CHIRI CHA MZIMU WOYERA. Ndipo adzabala mwana wamwamuna ndipo adzamucha dzina lache Yesu (Ambuye anapulumutsa)" - Mateyu 1:20-23.



KUMENE IYE ANACHOKERA MU PFUKO LA YUDA

Ulosi wa m'chipangano chatsopano:

"Ndodo yachifumu siidzachoka mwa Yuda,... kufikira atadza Silo, ndipo anthu adzamumvera iye." - Genesis 49:10.

Kukwanirtsidwa kwa ulosiu m'chipangano chatsopano:

"Pakuti kwadziwikadi kuti, Ambuye wathu anatuluka mwa Yuda." - Aheberi 7:14.

KUKANIDWA KWAKE

Ulosi wa m'chipangano chakale:

"Iye ananyozedwa ndi kukanidwa ndi anthu." - Yesaya 53:3. Kukwanirtsidwa kwa ulosiu m'chipangano chatsopano:

"Anadza kwa zake za lye yekha, ndipo ake amwini yekha sanamlandira lye." - Yohane 1:11.



KUPEREKEDWA KWAKE NDI MTENGO WA MALIPIRO APATSIDWA

Ulosi wa m'chipango chakale.

"Ngakhale Bwenzi langa lenileni, amene ndamkhulupirira , ndiyе amene adadyako mkate wanga, anandikwezera chidende chake." - Masalimo 41:9.

"Ndipo ndinanena nao, 'Chikakomera inu ndipatseni mphoto yanga; ngati iai, lekani. Ndipo anayesa mphoto yanga, kulemera kwake NDARAMA ZASILIVA MAKUMI ATATU." - Zakariya 11:12.

Kukwanitsidwa kwa ulosiu m'chipangano chatsopano:

"Pomwepo mmodzi wa khumi ndi awiriwo, dzina lake Yudase Isikariote, anamuka kwa ansembe akuru, nati, mufuna kundipatsa chiani, ndipo ine ndidzampereka lye kwa inu? Ndipo iwo anawerengera lye NDARAMA ZASILIVA makumi atatu." - Mateyu 26:14, 15.

IMFA YAKE PAMTANDA

Ulosi wa m'chipangano cha kale:

"Andi boola m'manja anga ndi m'mapazi anga." - Masalimo 22:16.

Kukwanirtsidwa kwa ulosiu m'chipangano chatsopano:

"Ndipo pamene anafika ku malo dzina lake Bade, Anampachika lye." - Luka 23:33 (*onaninso pa Yohane 20:25*).

KUCHOKA KWAKE M'MANDA

Ulosi wa m'chipangano chakale:

"Pakuti simudzasiya moyo wanga kumanda; simudzalola wokondedwa wanu abvunde." - Masalimo 16:10.

Kukwanirtsidwa kwa Ulosiu m'chipangano chatsopano:

"Iye pakuona ichi kale, analankhula za kuuka kwa Kristu, kuti sanasiyidwa m'hade, ndipo thupi lake silinaone



chibvundi. Yesu ameneyo, Mulungu anumuukitsa, za ichi tiri mboni ife tonse." - Machitidwe 2:31, 32.

Umboni wokwanira ndi wamphamu woti Yesu sanangopezekamo m'maulosiwa ayi. Mbiri ya moyo wake inalembedwadi kale kale chisanakhazikitsidwe chiri chonse. Zonna, Yesu ndi mwana wa Mulungu.

Titatha kuona umboniwi, tiyenera kupemphera popanga chisankho cha amene ayenera kukhala Ambuye wa moyo wathu. Ngati simunachite izi, kodi mungatero, kuika moyo wanu m'manja mwake?

4. MOYO WOKONZEDWERATU NDI MULUNGU

Yesu anakhala moyo womwe udali wokonzedweratu ndi Mulungu Zaka zambiri mbuyomo ye asanabadwe. Pokhudzidwa ndi izi, lye anakhala woganizira mwakuya pochita momwe Mulunguyo adamutsogolerera. Khristu anati:

"Ndipo sindicita kanthu kwa Ine ndekha, koma monga anandiphunzitsa Atate, ndilankhula izi,... chifukwa ndichita Ine zimene zimukondweretsa lye nthawi zonse." - Yohane 8:28-29.

Mulungu adakonzeratu moyo wa umunthu wa Yesu Khristu iye asanabadwe, ndi amakonzeratunso chimodzimodzi moyo wamunthu ali yense. Amadziwa mmene aliyense waife angakwanitsire zilakolako zake zakuya ndi kupeza moyo wathunthu.



Ray sanafike podziwa motsimikiza kwenikweni kuti apereke moyo wake kwa Mulungu. Koma atafika posankha za sukulu ya ukachenjede yomwe adayenera kupita, adafunsa chitsogozo cha Mulungu kwa nthawi yoyamba. Anapemphera kwa masiku angapo kudikira yankho. Patapita nthawi adafika pa chitsimikizo kuti ali ndi zifukwa zokwanira kusankha mbali B ya zomwe adayenera kusankhazo. Mbaliyi inali kunena za sukulu yochipa koma yaikulu kwambiri. Atapita ndipo atangoyamba kumene maphunziro aka adazolowerana kwambiri ndi a khrisitu ena ozizwitsa omwe anali a bungwe lina la pa sukulupo lotchedwa 'Ankhondo A Khristu'. Zomwe anapeza pokhala nawo kwa zaka ziwiri zinasintha moyo wake modabwitsa.

Pamene Ray ankayang'ana moyo wake wambuyo, anapeza kuti nthawi zonse ankapezana ndi chisankho chachikulu choti apange mwachitsimikizo napempha mphamu za umulungu kuti zimutsogolere, "Mulungu anatsegula zonse zatsopano za m'moyo wanga".

Kodi mungadziwe bwanji chikonzero cha Mulungu pa moyo wanu? Mulungu akutitsogolera mu njira zingapo:

(1) BAIBULO

"Mau anu ndiwo nyali ya kumapazi anga ndi kuunika kwa panjira panga." - Masalimo 119:105.

Wolemba masalimoyu wapeza choncho kuti buku lopatulika ndiye chitsogozo.

Mawu a Mulungu amakonzanso mwatsopano maganizo athu ndi kutipatsa chidziwitso (Aroma 12:12, Masalimo 119:99). Kuwerenga mauwa ndi kupemphera nthawi zonse ndiye njira yoposa zonse popezera zofunika zenizeni m'moyo wathu.

(2) NJIRA ZA ZOCHITIKA MOTIPATSA

Mulungu amatitsogoleranso potionetsera zochitika zoyeru zotitsogolera. Masalimo 23 akumuonetsera lye

ngati mbusa wabwino. Mbusa amatsogolera nkhosa zake mzigwa zoopsa ngakhalenso mmatanthwe ovuta. Amatha kuthandiza mntchito zake kuti zipindule ndi kuphunzitsa. Tiri ndi m'busa ife amene amakhala pafupi nafe nthawi zonse.

(3) KULANKHULANA KWACHINDUNJI NDI MTIMA KOMWE MULUNGU AMACHITA

Mulungu amatitsogoleranso poyankhula ndi maganizo athu a umunthu. Mzimu utha kutionetsera "maso athu a mumtima" (Aefeso 1:18). Nthawi zonse pamene tilumikizana ndi Mulungu, ndipamenenso amatha nayenso kutitsogolera. Anaumba zonse zathu, maganizo a mkaati mwamtimma wathu kuti tiwone choyenera chenicheni kuti tingachite nthawi zonse.

5. ZITSOGOZO ZIYENERA KUGWIRIZANITSA

Ndizotheka, ndithu, kuona ngati ukuyenda mmoyo wotsogozedwa ndi Mulungu pamene ukungotsatira za iwe mwini (Miyambo 16:25). Zofuna zathu ziyenera kugwirizana ndi ziphunzitso za mu baibulo. Sichanzeru kungoganiza Mulungu akutsogolera pokhapokha titaona kuti mitu itatu iri mwambayo ikuyendera limodzi.

Tamuoneni, mwachitsanzo, munthu uyu wotchedwa Jake. Analu ndi mkazi wake wokondeka ndi ana awiri, koma analinso ndi mkazi wina kumbali. Anawauza anzake: "Ndapemphera kwa Mulungu za izi ndipo ndikuona kuti ichi ndi chifuniro chake".

Maganizo a Jake ndi "Kumva kwake kwa mumtima" kumamutsogoza kunjira yolakwika. Iye anaona ndi kuganizira kuti chinali "chopatsidwa" kuti iye akumane ndi mkazi winayu ndipo sanabwererenco kukawerenga zomwe baibulo likunena ayi, pa za chigololo. Ndipo Baibulo, "ku chilamulo ndi umboni , ndilo bukhu lololedwa kutitsogolera, loyenera kutiuza choyenera chenicheni kuti tichichite (Yesaya 8:20).

Tisalole maganizo ena aliwonse kapena choperekedwa kwa lye chiru chonse kutitsogolera kuntchito motsutsana ndi mawu a Mulungu.

6. KUDZIPEREKA KU CHIKONZERO CHA MULUNGU

Yesu atalandira satana kuti amuyese m'chipululu, anamuonetsera izi, "ngati ungachite modzipereka podzipereka nsembe yopweteka yomwe Atate wakukonzena lwe, ndidzakupatsa dziko lonse lapansi m'dzanja lako udzachuka, udzakhala wamwayi, ndi moyo wofewa udzakhala ndi lwe". Satanayo anapereka umboni ndi mawu a m'bukhu lopatulika kuyesetsa kuti amusocheretse Yesu. Koma nthawi zonse Yesu anamugonjetsa ndi mawu akuti " kwalembedwa" (Mateyu 4:1-11).



Phunziro lalikuru ndi lamphamu lomwe tikuphunzira apa ndi moyo wa Yesu Khristu ndi lodzipereka ku chifuniro cha Atate. Ngakhale mkaati mwa zowawa za Getsemane, iye analira nati, "Atate ngati nkotheka, chikho ichi chindipitire, osati mwa kufuna kwanga ayi, koma mwa kufuna kwanu" (Mateyu 26:39). Patapita zaka zitatu za utumiki wake pokhala tsiku ndi tsiku mu mgwirizano ndi chikonzero cha Atate wake, Mawu omwe adayankhula pakufa anati, "Kwatha" (Yohane 19:30). Yesu apa amanena kuti, Chikonzero cha Atate pa moyo chafika kumapeto ndipo chakwanirtsidwa".

Pamene muyamba kumva liu la Mulungu kuyankhula nanu mosalekeza ndi mogwirizana m'mawu ake, zomwe watipatsa, ndi zokwaniritsa zake, mutha inu kuphunzira kumulandira ndi mtima wanu wonse mu ziphunzitso zake.

Inunso mutha kupeza chisangalalo cha chikonzero ndi chitsogozo cha Mulungu pa moyo wanu.

Nthano zonse zanenedwazi zikupeze ka mu zolemba za mpingo wa khristu momwe muli nthano za mbiri ya mpingo wakale.

ULALO WA KU MOYO WOKWANITSIDWA

Anapeza mafupa pambali pa denga la msasa wina wake pa chisumbu chapachokha pakati pa nyanja ya Atlantic.


Wapanyanja wopanda dzina uyu ankasunga zonse za zoledbedwa pa miyezi yake inayi yakukhala panyanja. Ananyamuka ulendo wake wapanyanja pa chisumbu cha kukwera ndi gulu la panyanja la ma Dutch muchaka cha 1725 chifukwa cha mulandu womwe sukutchulidwa. Posakhalitsa chifukwa cha ludzu lalikulu lamadzi, anafika pomwa mwazi wa a fulu a m'madzi. Kuvutika kwake kunali kwakukulu, koma chomupweteka kwambiri mwa zonse, monga mwa kulemba kwake, akuti unali: mlandu wa tchimo lake lalikuru.



Analemba mawu owawa ngati awa: "Kodi ndi kuwawa kotani komwe ochimwitsitsa amamva atasiyana nayo njira yachilungamo, nakondwera kuonjezera chiwerengero chaotayika". Wapanyanjayu ndikudzipatula kwake m'gulu pa chisumbu chapaokha chija kunabwera ndi maganizo ake akuti walekananso ndi Mulungu. Ndizomwe zinampangitsa kulephera kudzigmira ndi kudzivomera pa mapeto pake.

Anthu akhala akulimbana ndi kudzilekanitsa kwa mtimaku kuyambira pomwe Adamu ndi Hava "Anabisala kwa Ambuye Mulungu mu mitengo ya M'munda muja", atatha kudya chipatso choletsedwa chija (Genesis 3:8).

Chowawa cha mumtima chatsopano cha manyazi, kumva kulakika, ndi mantha zinawapangitsa anthu oyambirira awiriwa kuthawa pamene Mulungu anawaitana. Maganizo awa, mwatsoka, akupezekanso mwa ife lero. Kodi ndi chiyani chenicheni chopangitsa kuti ife tikalekane ndi Mulungu?



"Koma zoipa zanu zakulekanitsani inu ndi Mulungu wanu; ndipo machimo anu abisa nkhopre yace kwa inu." - Yesay 59:2.

Choipa chachikuluchi cholekanitsa anthu ochimwa ndi Mulungu waho sichiri chikonzero cha Mulungu ayi: Mulungu sanamuthaweho Adamu ndi Hava - iwo ndiwo adamunthaweho.

1. KUKWANITSA NJALA YATHU YOBISIKA

Tchimo lisadaononge chithunzichi, Adamu ndi Hava anali mchisangalalo cha ubale ndi Mlengi waho m'munda wokongola kwambiri wa Edeni komwe kunali kwao. Mwatsoka, anatenga bodza lonyengerera la Satana loti iwo adzakhala ndi nzeru ngati Mulungu, lomwe linaphwanya mgwirizano wokhulupirirana ndi wowapangayo (Genesis 3).

Atachotsedwa m'munda wa Edeni, Adamu ndi Hava anakhala moyo wowawa kunja kwa mundawo - kuberekana, ndi kulima mnthaka tsopano kunadzetza mwazi, thukuta ndi misozi. Ubale waho ndi Mulungu utasweka, anapezeka ndi zilakolako zosakwanitsika ndi zilandiro zowawa - undekha wa tchimo.

Kuyambira pamene Adamu ndi Hava adagalukira pachiyambi, "Onse" (Mtundu wonse wa anthu) unagwa mundondomeko yomweyi ya tchimo nakhala nawo mu mzere woti adzafa, chomwe chiri mphotho yake ya tchimo.

"Chifukwa chake monga uchimo unalowa m'dziko lapansi mwa munthu m'modzi, ndi imfa mwa uchimo, CHOTERO IMFA INAFIKIRA ANTHU ONSE, Chifukwa kuti onse ANACHIMWA." - Aroma 5:12.



Tonse tidakhala nawo machitidwe a njala ya zofuna za mtima pa zomwe tidataya, kufunafuna chitetezo chokhacho chomwe Mulungu yekha angapereke. Nthawi zambiri timafuna kudzikwaniritsa pogula zambiri zochitira maphwando, pofuna kukwera m'maudindo pa ntchito, kapena kuthetsa njala zathu ndi a vinyo osasa, mankhwala osokeneza bongo ndi madama. Koma zonezi zisonyeza makhalidwe athu osoweka Mulungu. Palibenso machiritso ena ku izi oposa kupeza nawo chikondi chake m'moyo wathu.

"Inu... pankhope panu pali chimwemwe chokwanira; m'dzanja lanu lamanja muli zokondweretsa zomka muyaya." - Masalimo 16:11.

2. KULUZANITSA PHANGA LALIKURU LA TCHIMO NDI IMFA

Sianthu okha amene amaoneka osungulumwa chifukwa cha tchimo. Mtima wa Mulungu unapwetekanso panthawi yomwe Adamu ndi Hava adamfulatira lye. Ndiponso lye amamvabe chisoni ndi matsoka a munthu. Mulungu ndi wolola ndi wofunitsitsa kukhutitsa zofuna zathu zobisika ndi kupoletsa mabala a kusweka kwa maganizo a mumtima mwathu. lye sanakwanitsidwe ndi kuona mwachisoni kokha pa phanga lalikulu limene lalekanitsa ife ndi lye ayi. Mulungu anatsimikiza kukhala ulalo pakati pa phangali ndi imfa.

"Pakuti Mulungu anakonda dziko lapansi kotero kuti anapatsa mwana wake wobadwa yekha, kuti yense wakukhulupirira lye asatayike , koma akhale nawo moyo wosatha. Pakuti Mulungu sanafuna mwana wake kudziko lapansi, kuti akaweruze dziko lapansi, koma kuti dziko lapansi, likapulumutsidwe ndi lye." - Yohane 3:16, 17.

Mulungu anapereka mwana wake, ndipo Yesu anapereka moyo wake ngati nsembe ya tchimo, kulipira imfa iye mwini. Moyo wake, imfa yake, ndi kuuka kwake kunapangitsa kuti tchimo litha kukhululukidwa ndi kupulumutsa wochimwayo mopanda kulichepetsa tchimolo; ndipo dziko lapansi linalandira chitsanzo cha khalidwe lake lenileni la Khristu ndi Satana.

Ulalo wa thupi lotundudzidwa, lokha mwazi wa Yesu Khristu, limakokera anthu kuchokera ku misampha ya tchimo.



Chikondi chimakwirira phangali, kuwapangitsa onse okhulupirira mwa Khristu ngati Ambuye ndi Mpulumutsi kuyenda m'moyo wosatha.

2. MFUNDO ZISANU NDI ZIWIRI ZOFUNIKA KUZIDZIWA ZOKHUDZA YESU

Mfundozitu sizoona kwa munthu aliyense amene adakhalako:

- YESU ANACHOKERA KUMWAMBA KUDZA PADZIKO LAPANSI
Kodi Yesu amati wakhala zaka zingati?

"Asanabadwe Abrahamu Ine ndiripo." - Yohane 8:59.

Yesu analidziwitsa dziko lapansi: "Ndine"! Ndakhalako kuyambira kale ndipo ndidzakhalakobe. Ngakhale Yesu anabadwira mwa mayi wa umunthu (Mateyu 1:22, 23) lye ndi Mulungu - Mulungu mwa munthu.



Dwight L Moody, yemwe ndi Billy Graham wa mu zaka za mazana khumi ndi anayi, (19th Century) nthawi ina ananenapo za umunthu wa Yesu Khristu kuti, " Ikanakhala nsembe yaikuru kuti Yesu abwere ndikubadwira muchobadwira cha siliva, nasamalidwa ndi angelo, nadyetseredwa ndi ng'ombe ya golide. koma mlengi wa kumwamba ndi dziko lapansi anadza nakhala ndi thupi la umunthu, nabadwira mkhola, mwa makolo osauka ndi munyengo ndi malo oipa.

M'ngelo anamuua Yosefe pa nthawi ya kubadwa kwa Yesu:

"Ndipo (Mariya) adzabala mwana wamwamuna, ndipo udzamucha dzina lake Yesu, pakuti IYEYO ADZAPULUMUTSA ANTHU ACHE KU MACHIMO AO." - Mateyu 1:21.

Yesu, Mlengi wa dziko lapansi (Yohane 1:1-3, 14), anali wolola kudza ku dziko lapansi kudzapulumutsa ife kumachimo ndi imfa.

(2) YESU ANAKHALA MOYO WOSACHIMWA

"Yesu Mwana wa Mulungu,... wayesedwa m'zonse monga momwe ife - koma wopanda uchimo." - Aheberi 4:14, 15.

Mulungu anachita zambiri zoposa kungotiuza ife za kuchoka ku moyowu wa tchimo kupita ku moyo wokwanitsidwa. Pokhala nafe ngati munthu, Yesu anaupanga moyo wopanda tchimo, ndiwosiririka moti palibenso ulaliki womwe ukonaththa kuonetsera izi motere.

Satana, mdani wa Khristu, anakonza chiwembu mu moyo wake wonse wa Yesu kuti amugwetse lye mu tchimo. Mu chipululu, Satana anachita mbali yake yonse yantchito yake yoopsyta yothetsa ulemu wake wa Khristu (Mateyu 4:1-11). Mu Getseman, lye asanapachikidwe, mayesero anamfikira kwakukuru kufikira kuturutsa thukuta la mwazi (Luka 22:44).

Koma Khristu anaima njilu ku mayesero onse mdirekezi anamukonzera - "Wopanda kuchimwapo". Chifukwa chakuti Yesu anakumana nawo uthunthu wonse wa mavuto ndi mayesero, amamvetsetsa za kuvutika kwathu poyesetsa. Amatha "Kumva nafe chisoni pa kufooka kwathu" (Aheberi 4:15).

Zinatheka bwanji kuti Yesu akhale moyo wopanda tchimo?

"Ameneyo sanadziwa uchimo anamuyesera uchimo m'malo mwathu; kuti ife tikhale chilungamo cha Mulungu mwa lye." - 2 Akorinto 5:21.

(3) YESU ANAFA KUTI ACHOTSE TCHIMO
Kodi ndi anthu angati amene anachimwa?

"Pakuti onse anachimwa, naperewera pa ulemerero wa Mulungu." - Aroma 3:23.

Nanga mphotho yake ya uchimo ndi chiyani?



"Pakuti mphotho yake ya uchimo ndi IMFA, koma mphatso yaulere ya Mulungu ndiyo moyo wosatha mwa Khristu Yesu Ambuye wathu." - Aroma 6:23.

CHIFUKWA CHIYANI YESU ANAFA?

"Taonani, Mwana Wankhosa wa Mulungu, amene ACHOTSA MACHIMO a dziko lonse lapansi" (Yohane 1:29).

Tonse tinachimwa ndipo tiyenera imfa yosatha, koma Yesu anafa m'malo mwathu. Anasanduka "Tchimo kwa Iye". Analipira dipo lathu. Kufa kwake kuli mphatso, ndi "MPHATSO ya Mulungu ndi moyo WAMUYAYA kwa Khristu Yesu Ambuye wathu" (Aroma 6:23).

Yesu anasiya ungiro wake, moyo wake wachilungamo ngati mphatso yachikondi kwa ife. Chikondi chotere ndichoti munthu sangachimvetsetse. Ndipo chifukwa cha imfa yakeyi "tiri ndi MTENDERE ndi Mulungu" (Aroma 5:1).

(4) YESU ANAUKA KWA AKUFA

Imfa ya Yesu pa mtanda sanali mapeto ambiri yake yodabwitsa ayi. Sakanakhala wakufa nakhalabe Mpulumutsi wathu.

"Ndipo ngati Khristu sanaukitsidwa, chikhulupiro chanu chiri chopanda pache; muli chikhaliire m'machimo anu. Chifukwa chake iwonso akugona mwa Khristu anatayika." - 1 Akorinto 15:17, 18.

Muhamadi ndi Buda aphunzitsa ziphunzitso zina zazikuru ku dziko lapansi. Ndipo akhudza miyoyo zikwizikwi ya anthu ndi uthenga wawo, koma alibe mphamvu zodabwitsa zakupereka moyo. Ndichifukwa onsewa adakali m'manda mwawo.

Ndi chifukwa chiyani Yesu anauka m'manda pa tsiku lachitatu kuchokera pomwe anafa, nanga ndi lonjezano liti lomwe akufuna kupanga kwa ife?

"Popeza Ine ndiri ndi moyo inunso mudzakhala ndi moyo." - Yohane 14:19.

Yesu ali wa moyo! Chifukwa ali ndi mphamvu zogonjetsera imfa ndi kupereka moyo womwe uli wamphumphu ndi wosatha. Adzakhala mu mtima mwathu ngati timuitana. Khristu woukitsidwayo alipo lero kukumana ndi zosowa zathu.

"Ine ndiri pamodzi ndi inu masiku onse, kufikira chimariziro cha nthawi ya pansi pano." - Mateyu 28:20.

Amuna ndi akazi padziko lonse lapansi akugawana nawo nthanoyi ya m'mene Khristu wawachotsera kuwapulumutsa ndi kuwamasula ku zizolowezi zoipa za moyo uno.

M'modzi wa aphunzi akale adalemba mawu awa oyamikira pa limodzi la mapepala ake a mayankho: "Ndinali chidakwa. Tsiku lina ndiri chiledzelere, ndinapeza chikalata cholengeza za maphunziro anu a baibulo mu malo oyenda madzi. Ndinalitenga pepalalo, nandilembapo, nandiyamba kulandira chidziwitso choona choyamba cha Khristu. Nditanotsiriza maphunzirowa ndinapereka moyo wanga kwa Mulungu ndikusiya moyo wauchidakwawo".



Pamene Yesu anatenga ulamuliro wa moyo wa munthuyu, mphamvu ina yake yatsopano inampatsa lye mphamvu yogonjetsera zizolowezi zake. Pakuti Khristu ndi Mpulumutsi woukitsidwa, adzapulumutsa aliyense wodza lye kufuna chithandizo.

(5) YESU ANAKWERA KUNKA KUMWAMBA

Yesu atangouka kwa akufa asanakwere kubwerera kwa Atate (Machitidwe 1:9), anapereka lonjezo iri kwa omutsatira lye:

"Mtima wanu usabvutike; mukhulupirira Mulungu, khulupirirani inenso. M'nyumba ya Atate wanga alimo malo okhalamo ambiri;... ndipita KUKAKONZERANI INU MALO. Ndipo ngati ndipita kukakonzera inu malo... ndidzabweranso ndipo ndidzalandira inu kwa Ine ndekha... kumene kuli ineko. Mukakhale inunso." - Yohane 14:1-3.

(6) YESU AKUTUMIKIRA MONGA WANSEMBE WAKUMWAMBA
Yesu nthawi zonse amayesetsa kufufuza kupeza motikonzetsera malo kumwamba.



"Potero kudamuyenera kufanizidwa ndi abale m'zonse, Kuti akadzakhala mkulu wa ansenbe wachifundo ndi wokhulupirika m'zinhu za kwa Mulungu, kuti apereke dipa la zoipa za anthu. pakuti popeza adamva zowawa, poyesedwa yekha, akhoza kuthandiza iwo amene ayesedwa." - Aheberi 2:17-18.

Yesu anadza ku dziko lapansi "Kudzapereka dipa lake la chimo za anthu". Ndikuwapulumutsa iwo kuchokera ku Zisoni za ukapolo wa machimowo. Anafa kutipulumutsa kuti akathetse zomwe ziyambitsa tchimo, kuzunzika, ndi imfa pomuphwanya mdierekezi.

Yesu, wansembe wathu wamkulu "aNapangidwa mu zonse monga abale ake". Ndipo pano akuonekera pamaso pa Atate mmalo mwathu ngati wotimirira. Yesu yemwego yemwe anadalitsa ana anapulumutsa ndi kumukonzanso mayi wogwidwa ndi chigololo, nakhululukira mbala yofa pamtanda; akugwira ntchito panopa kumwamba kukwaniritsa zosowa zathu "kuthandiza iwo amene akuyesedwa".

(7) YESU ADZABWERANSO YESU ASANABWERERE KUNKA KUMWAMBA, ANALONJEZA CHIYANI?

"Ndipo ngati ndipita kukakonzera inu malo, 'ndidzabweranso' ndipo ndidzalandira inu kwa Ine ndekha, kuti kumene kuli Ineko, mukakhale inunso." - Yohane 14:3.

Yesu podzabwera, adzatimasula ife ku chimo, matenda, matsoka ndi imfa zomwe zabvutitsa dziko lapansi. Ndipo adzatilandira ife ku dziko latsopano chisangalalo cha muyaya ndi moyo wosafa.

4. CHIKONDI CHOSALEPHERA

Nthano ikunenedwa ya ukwati womwe unakonzedwa ku Taiwani pakati pa U Long ndi msungwana dzina lake "Golden Flower". Pamene U Long anavundukula chofunda chakumutu cha mkwatibwi wake utatha mwambo wokwatitsidwa, anazizwa modabwitsika kuona kuti nkhopre yonse ya mkaziyo inakutidwa ndi zipsera za nthomba.

Zitatha choncho, U Long analibe nayenso chidwi mkaziyo. Anayesetsa mkaziyo kumukondweretsa U Long pogwira ntchito molimba panyumba ndi chiyembekezo choti mwamuna wake anconde momwe aliri. Koma iye anakhalabe wosayamikira machitidwe a mkazi wakeyu.

Patatha zaka khumi ndi ziwiri a banja lotereli, U long anayamba kusaonetsetsa bwino. Madotolo pumuyeza adamuuza iye kuti tsiku lina adzakhala wa khungu ngati sangatthe kukaiktsa choonera china cha mdisomo chatsopano. Koma kuikitsako ndi ntchito yakeyo zinali zofuna ndalamama zambiri koposa komanso panali mndandanda wa anthu ambiri ofuna chithandizo chomwechi asanafike iye.

Mkazi wake, Golden Flower anayamba kugwira ntchito nthawi yaitali patsiku kupanga zisoti za mulaza kuti apeze ndalamama zoonjezera. Tsiku lina, U Long anauzidwa kuti wina wake ali ndi chamdiso chomwe iye akuchifuna chija anathamangira kuchipatala kuja komwe anakamupanga opereshoni.

Atachira, adadzikakamiza mwazifukwa kuti aonane ndi mkazi wake kuti amuthokoze iye poyesetsa kupeza ndalamama. Pamene mkaziyo anatukula mutu wake kuti amuyang'ane mwamuna wake anamuona iye wakhungu, maso opanda kanthu, chiwalo chofunika chija choyerha cha diso chitachoka, akuthatha. Atakhudzidwa ndi chisoni, anabisa nkhope yake nayamba kulira. Kwa nthawi yoyamba U Long anaitana monong'ona dzina la mkazi wake : Golden Flower.



Yesu akufufuza ubale ndi iwo amene amkayika lye namutsutsa kwa nthawi yaitali; Akufuna ife kuti pamapeto pake tiitane monong'ona dzina lake ndi kulitchula ngati mpulumutsi wathu. Lye anali wolola kupereka moyo wake nsembe osati maso ake okha ayi koma thupi lake lonse kuonetsera chikondi chake chosalephera. Chikondi chake ndi champhamvu koposa kotero kuti Khristu "anadza ku dziko kudzapulumutsa wochimwa" (1 Timoteo 1:15).

Nsembe yaikulu ya Khristu yabweretsa ulalo womwe walunzanitsa kusiyana maganizo kwathu, komwe kwakuta kupunduka kwathu. Kodi inu panokha, mwapeza kuti iye akufuna kukudutsitsani inu dzenjeli kuti mugwe m'manja ake? Mungavomere ndi kupemphera kuti, "Yesu, ndimakukondani. Zikomo chifukwa cha chikondi chanu chodzipereka nacho nsembe. Idzani mu mtima mwanga ndi kundipulumutsa ine ndense, kwathunthu ndi kwamuyaya?"

YESU

Anadza ngati Mulungu mwa Munthu
 Anakhala moyo wopanda tchimo mmalo mwa ife
 Anafera zochimwa zathu
 Anauka kutiomboloa ife kuimfa
 Anakwera kumwamba kukatikonzeru mudzi wokhalako
 Akutumikira tsiku ndi tsiku ngati wansembe wantru wamkuru
 Akubwera posachedwa kudzatitenga ife kuti tikakhale ndi lye kwa tuyaya

MWAYI WOKHALA MOYO WA CHIWIRI

Munthu wina wokalamba atatha kukhala moyo wake wonse m'chipembedzo cha chi Buda, nasankha kukhala mkhristu ku dziko la Singapore, anafunsidwa, "kodi inu Mr. Lim, mukupeza kusiyana kwa mtundu wanji pakukhala mkhristu ndi kukhala m'Buda?

"Ndikosavuta," anayankha choncho. "kuyambira pomwe ndinapeza Yesu ngati mpulumutsi wanga ndiri ndi mtendere waukuru mu mtima. Izi ndi zomwe zimachitika tikaika moyo wathu pa Khristu.


"Inu (Mulungu) mudzasunga mtima wokhazikika mu mtendere weni-weni chifukwa ndikhulupilirani inu," - Yesaya 26:3.

Kukhala moyo wachikhristu kumadzetsa mtendere wangwiro - kumva chitetezo chokhala bwino ndi changwiro. Iwo amene apeza chisangalalochi angopezeratu njira yokhayo ya ku mwayi wokhala moyo wachiwiri - Yesu!

1. TANTHAUZO LA KUPULUMUTSIDWA KWA IWO WOTAIIKA

Nzotheka kuti munthu wa moyo wake wathanzi kukhala ndi moyo ndi nthawi yomwe ena angaitchule kuti ndiyabwino, koma ali wakufa - kufa kuuzimu.

"NDIPO INU, ANAKUPATSANI MOYO, pokhala munali akufa ndi zolakwa, zimene munayendamo kale, monga mwamayendedwe a dziko lapansi lino, monga mwa mkuru wa ulamuliro wa mlenga-lenga, wa mzimu wakuchita tsopano mwa ana a kusamvera." - Aefeso 2:1, 2.



Satana amatsoglera munthu wakufa muuzimu kuti agwebe mu uchimo ndi kusamvera. Koma choonadi chozizwitsa cha uthenga wabwino ndichakuti Mulungu amawakonda anthu oterewa. Iye amawakonda anthuwa adakali chichimwire, nawapatsa chipulumutso chaulele ndi chodzaza ku machimo awo.

"Chifukwa cha chikondi chake chakuya chimene anatikonda nacho, Mulungu, wodzala ndi chifundo, tingakhale tinali akufa m'zolakwa zathu, anatipatsa moyo pamodzi ndi khristu (muli opulumutsidwa mwa chisomo)... kuti akaonetsera m'nyengo zirinkudza chuma choposa cha chisomo chake, m'kukoma mtima kwa pa ife mwa Khristu Yesu." - Aefeso 2:4-7.

Mulungu anatikonda ngakhale pamene sitinali woyenera kukondedwa. Chisomo chake chinalenga m'miyoyo yathu, moyo watsopano wa khristu. Sitingathe kuzisinta tokha ayi, koma Mulungu akhoza. Tikabwera kwa lye ndi chikhulupiliro ndi kudzipereka, amatipatsa ife mwayi wina wachiwiri ngati mphatso yaulele pa moyo wathu.

2. TIYENERA KUPULUMUTSIDWA KU CHIYANI?

(1) Tiyenera kupulumutsidwa ku tchimo.

"Pakuti onse anachimwa, naperewera pa ulemelero wa Mulungu." - Aroma 3:23.

Kunena mwachuchuchu, ife sitikhala moyo umene tinafunikira mwa ubwino. Kholo litha kupsa mtima ndi kum'pweteka mwana wake chifukwa mavuto ambiri Omwe avutitsa m'moyo wake. Munthu atha kukhala

ndi chidwi pa woyendetsa galimoto mpaka kutsala pang'ono kuchita ngozi. Ophunzira atha kukhala wosathandizika nanena mau oipa pa za ophunzira mzake. Wochita malonda atha kukonza "kuti aiwale" za komwe kuchokera chuma chake nthawi ya msonkho. "Onse anachimwa," ndiye momwe munthu aliri m'menemo.

Kodi baibulo likutanthauzira bwanji tchimo?

"Chosalungama chiru chonse chiru uchimo," - 1 Yohane 5:17.

Tiyenera ife kupulumutsidwa ku makhalidwe onse oipa, monga bodza, mkwiyo woononga, zilakolako, kupsa mtima, ponganena zochepa.



"Yense wakuchita chimo achitanso kusaweruzika." - 1 Yohane 3:4.

Choncho tiyenera kupulumutsidwa ku tchimo loswa Malamulo ake a Yehova.

(2) Tiyenera kupulumutsidwa ku ubale wosweka umene ulipo ndi Mulungu.

"Koma zoipa zanu zokulekanitsani inu ndi Mulungu wanu; ndipo machimo anu abisa nkhope yake kwa inu kuti lye sakumva." - Yesaya 59:2.

Tchimo lomwe silinakhululukildwe limachotsa ubale ndi Mulungu. Khristu anadza kudzabwezera chikhulupiliro mwa Mulungu, chimene satana anachisokoneza kuchichepetsa.

(3) Tiyenera kupulumutsidwa ku imfa yosatha chilango cha -mphotho ya utchimo.

"Chifukwa chake, monga uchimo unalowa m'dziko lapansi mwa munthu m'modzi, ndi imfa mwa uchimo, chotero imfa inafikira anthu onse, chifukwa kuti onse anachimwa." - Aroma 5:12.

(4) Tiyenera Kupulumutsidwa kumoyo wosakondwa, wopanda pache wa uchimo.

Kwa ochimwa, moyo ndi njira yokathera ku imfa basi.

(5) Ife tiyenera kupulumutsidwa ku dziko lodzala ndi uchimoli ndi zotsatira zake za machimowo-monga kukhala wosangalala, kusweka mtima, kukhala pa uwekha, nkondo, matenda ndi imfa!

3. ANGATIPULUMUTSE NDANI?

(1) Yesu angatiombole ife ku tchimo.

"Ndipo udzamutcha dzina lake Yesu, pakuti iyeyu adzapulumutsa anthu ache ku machimo awo." - Mateyu 1:21.

Munthu wina wa chi Hindu anauza mzake wa chikhristu, "ndapeza zinthu zina zambiri mu chi Hindu zomwe sizipezeka mu chikhristu, koma pali chinthu chimodzi m'chikhristu chomwe mu chi Hindu mulibe. Ichi ndi Mpulumutsi.

Chikhristu ndi chipembedzo chokhacho m'dziko lapansi chomwe chimapereka kwa anthu Mpulumutsi.

(2) Yesu atha kutipulumutsa ku ubale wathu womwe udasweka ndi Mulungu.

"Kuti nthawi ija munali opanda Khristu... opanda chiyembekezo, ndi opanda Mulungu m'dziko lapansi. Koma tsopano mwa Yesu Khristu inu amene munali kutali kale, anakusendezani mukhale pafupi m'mwazi wa Khristu." - Aefeso 2:12, 13.



Yesu ndiye bwenzi langwiro yemwe tingakhale naye mu ubale wa chisangalalo.

Anakonda kutibweretsera ife zabwino zokha-zokha. "Kupyolera m'mwazi wa Khristu"moyo wathu wakale wamachimo unakhululukidwa, ndipo tsiku ndi tsiku amatilandira ndi kutivomereza ife kutipatsa moyo wake wangwiro. Tikudziwa kuti alipo nthawi zonse kutidzutsa pamene tagwa. Chikondi chathu paiye chimatsatira pobwera chikhumbo-khumbo chokhala mu njira yom'kondweretsa lye.

(3) Yesu atha kutipulumutsa ku imfa ya tuyaya yomwe ndi mphotho yache ya uchimo.

"Pakuti mphotho yake ya uchimo ndi imfa; koma mphatso yaulele ya Mulungu ndiyo moyo wosatha wa mwa Khristu Yesu Ambuye wathu." - Aroma 6:23.

Ife ndife oswa lamulo oyenera imfa. Mphotho ya uchimo ndi imfa. Yesu anatipulumutsa ife ku imfa yamuyaya natipatsa ife moyo wosatha.

"Koma Mulungu atsimikiza kwa ife chikondi chake kwa chikondi chake cha mwini yekha, m'menemo kuti pokhala ife chikhaliere ochimwa, Khristu adatifera ife." - Aroma 5:8.

Chifukwa cha chikondi chosalephera, Yesu "anatifera ife." Ndiponso chifukwa anatifera ife nazunzidwa ndi mphotho yonse ya tchimo, Mulungu atha tsopano kukhululuka ndi kulandira wochimwa popanda kuchepetsa tchimolo.

(4) Yesu angatipulumutse ife ku moyo wosakondwa, wauchimo.

"Chifukwa chake ngati munthu ali yense ali mwa Khristu, ali wolengedwa watsopano, zinthu zakale zapita, taonani zakhala zatsopano." - 2 Akorinto 5:17.

Sitingathe ife kudzipulumutsa ife kudzipulumutsa tokha ku tchimo kapena kudzisinha tokha monga m'mene sizingakhalire zotheka mkango kusanduka khoswe (Aroma 7:18). Tchimo ndi lamphamvu kuposa maganizo athu. Koma Khristu atha kulimbikitsa inu ndi mphamvu mwa Mzimu wake mwa inu" (Aefeso 3:16). Iye amagwira ntchito yobwezera moyo wake wabwino m'malo amene khalidwe lathu linaonongeka; khalidwe labwinolo ndilo chikondi, mtendere, chisangalalo, chifatso ndi kudziletsa (Agalatiya 5:22, 23). Khristu amakhala moyo wake wonse mwa ife, ndipo timalandira machiritso a uzimu kubwezeretsedwanso mwatsopano ndi moyo watsopano.

Munthu wina wotchedwa Harold Hughes anataya chikhulupiliro chake kuti iye angathe kukhala wosinthika. Anayesa kusiya uchidakwa kwa nthawi yaitali koma analephera. Anaona kuti uchidakwa wake wazunzitsa mkazi ndi ana ake kwa zaka khumi. Ndiye tsiku lina analowa mu bafa losambira natenga mfuti yake nazilozetsa nayo mkamwa mwake.

Asanailole kuti imuombere, anaganiza zomulongsolera kaye Mulungu vuto lakeli. Pemphero lakeli linasandulika kudandaulira kolira kwakutali, kulilira chithandizo. Ndipo Mulungu anabwera. Harold Hughes anapanga chitsimikizo chake ndi Khristu naapeza mphamvu za uzimu zomwe zinamuthandiza kupilira. Anasiiratu moyo wauchidakwa, nasandulika bambo wachikondi, ndi wodalirika ku banja lake ndipo anapeza mpando wa udindo mu nyumba ya Malamulo ya "Senate." Harold Hughes anapeza mphamvu yoposa zonse yakumusintha munthu m'dziko lino lapansi - ndiyo Yesu!



(5) Yesu angatipulumutse ku dziko la uchimo.

Mitu ya maphunziro athu a kupeza mwatsopano anayi otsatirawa adzatifotokozena m'mene Yesu amapulumutsira anthu ku dziko lauchimo.

4. TIMAPULUMUTSIDWA NGATI TITHA KUCHITA ZINTHU ZITATU ZOSAVUTA IZI

(1) Kumufunsa Khristu kuthana ndi tchimo liri m'moyo mwathu.
Kodi ife mbali yathu ndiyotani pakuchotsa moyo wathu wauchimo?

"Lapani, bwelerani kuti afafanizidwe machimo anu." - Machitidwe 3:19.

"UBWINO WA MULUNGU UKUBWEZERA KUTI ULAPE." - Aroma 2:4.

"MWAMVETSEDWA CHISONI KU KUTEMBENUKA MTIMA." - 2 Akorinto 7:9.

Kulapa ndiko kumva chisoni ndi moyo wathu wakale wauchimo, ndikutembenuka mtima kuchoka ku chimolo; kusiya makhalidwe onse akale, ndi maganizo akale. Sichisoni chifukwa chongoopa chilango ayi, koma yankho lathu la kwa Mulungu ndi chifundo chake,' chomwe chinatsogolera Yesu kufa m'malo mwathu chifukwa cha machimo athu. Timakana tchimo chifukwa limamupweteka Mulungu.

Tikapeza moyo watsopano mwa Yesu Khristu, tiyenera kuyesetsa kusiya zonse zakale zoipa (Ezekiel 33:14-16).

Kodi ndi mbali yanji yomwe Mulungu ali nayo kuichita pochotsa moyo wathu wakale wauchimo?

Kulapa ndi kukhululukidwa; zonsezi ndi mphatso za Mulungu kwa ife.

"Ameneyo Mulungu anamkweza ndi dzanja lace lamanja, akhale mtsogoleri ndi MPULUMUTSI, kuti apatse kwa Israyeli KULAPA, ndi CHIKHULUPIIRO CHA MACHIMO." - Machitidwe 5:31.

Ndipo tikalapa, mpulumutsi wokondayo amatikhululukira machimo athu, natiyeretsa ife kumachimowo nawaponya kunyanja yakuya.

"NGATI TIVOMEREZA MACHIMO ATHU, ALI WOKHULUPILIKA NDI WOLUNGAMA IYE, KUTI ATIKHULULUKIRE machimo anthu ndi KUTISAMBITSA Chosalungama chonse." - 1 Yohane 1:9. (Onaninso pa Mika 7:18, 19.)

Palibe tchimo loopsa loti Mpulumutsi yemwe anafera machimo athu pa mtanda wa Karavali sangathe kukhululukira. Munthu amene akhulupilira mwa Yesu angofunika kumufunsa lye, Yesuyo kuti amukhululukire. Kufa kwa Yesu, kufera ife sikungatipulumutse pamene ife sitinapemphe ayi.

Ndizosakaikitsa kuti machimo athu ndiwo adapangitsa misomali ija kuboola thupi lake la Khristu paja pa mtanda, m'manja ndi m'mapazi ake.



Komabe Yesu akufunitsitsa, koposa m'mene tingaganizire kuti ife tilandire mphatso yakeyi ya kukhululukidwa ndi chiyanjano mwa iye.

Mawu adamufikira m'nyamata wina, yemwe adathawa kunyumba kwawo, kuti mayi ake ali pafupi kufa. Nkhaniyi inamuchititsa chisoni kwambiri poonanso ubale wake wosweka ndi banjali. Akufulumira kupita kunyumbako, anakadzigwetsa m'chipinda pa kama pomwe panagona

mayi akewo ndi misozi, akulira mopempha kuti mayi akewo amukhululukire.

Mayi adamusendeza iye pafupi nawo namunong'oneza mawu awa, "mwana wanga, ndikadakhala nditakukhululukira kale ukadandipempha koter."

Ngati inu mwapita kutali ndi Mulungu - Kapena simunamudziwebe - chonde, ganizirani momwe lye aliri ndi chidwi chokulandirani ngati Atate wokonda akufunitsitsa ndithu koposa zonse kuti inu mulandire mphatso yake yakukhululukira. Yesu amakukondani. Anafera inu. Ali wolola nthawi zonse kukukhululukirani choncho, inunso muvomereni ku kuitanira ku kulapa kwake. Lapani machimo anu. Mungokhulupira basi kuti Mulungu akukhululukirani ndipo achitadi. Mkhulupirireni lye! Khulupilirani malonjezo ake.

(2) Landirani moyo watsopano kuchokera mwa Yesu.

Mbali yanu polandira moyo watsopano kuchokera kwa Yesu ndikungokhupilira basi kuti Yesu wakupulumutsani inu. Vomerani popanda kung'ung'udza mfundo yoti lye wakukhululukirani, ndikukuyeretsani, kutenga zonse zanu zakale zauchimo, ndikukupatsani moyo wonse weni-weni watsopano wosinthika.

"Koma onse... okhulipilira dzina lake, kwa iwo anapatsa (mphamvu, undindo, mwayi) wakukhala ana a Mulungu." - Yohane 1:12.

Monga mwana wa Mulungu, muli ndi "ufulu" wakulandira moyo watsopano kuchokera kwa Yesu. Monga tanena kale, simungathe inu kuchita izi mwa inu nokha - izi ndi mphatso yochokera kwa atate wanu wakumwamba! Yesu amapereka lonjezano leni-leni ili kuti akatichotsere ife mantha akusoweka chitetezo ndi kukaika.

Kodi Mulungu amachitapo mbali yanji potipatsa ife moyo watsopano?

"Yesu anayankha nati; "Indetu indetu ndinena ndi iwe, ngati munthu sabadwa mwatsopano, sakhoza kuona ufumu wa Mulungu." - Yohane 3:3.

M'malingaliro a Yesu, wochimwa wokhulupilira ndikulapa ali wobadwanso mwatsopano m'moyo. Ndichoziwa chomwe angachichite ndi Mulungu yekha basi. lye akulonjeza:

"Ndipo ndidzakupatsani MTIMA WATSOPANO, ndi kulonga mkatı mwanu MZIMU WATSOPANO, ndipo ndidzachotsa mtima wamwala m'thupi, ndikukupatsani mtima wamnofu." - Ezekiel 36:26.

Yesu amasinha mitima yathu - maganizo ndimakhalidwe athu - ndipo amakhala "mwa ife" (Akolose 1:27). Moyo watsopanowu siwodzala ndi zabwino zokha-zokha zauzimu ayi, ndiwovuta, kuuka kuchoka ku imfa yauzimu kunka ku moyo wonse watsopano ndi kuhala munthu wokhalako weni-weni.

(3) Moyo wa chikhristu umafuna tsiku liri lonse kumachoka ku kudzikonda, ndikulumikizana ndi Yesu bwenzi lathu lokonda. Timakula m'moyo watsopanawo pakulimbikitsa ubale wathu ndi Yesu. Izi zitanthauza kutenga nthawi yathu yaitali ndi iye, kumanga naye m'gwirizano woona ndi wapoyer.

Mulungu watipatsa zotitsogolera zopatulika zisanu kuti zitithandize kukula mu uzimu. Zinthuzi ndi: Kuwerenga mawu ake m'baibulo, pemphero, kuchita monga mwa mawu ake, kukhalira pamodzi ndi anzathu mukupembedza, ndi kugawana nawo anzathu zomwe tapeza.

Kukhala mwa khristu sikutanthauza kuti sitingalakwitse zinthu ayi. Koma tikaphunthwa ndi kuchimwa, timaitanitsa chikhululukiro kwaYesu, ndikupitabe chitsogolo. Ife talunjikitsidwa ku njira ina yake ndipo tidziwa kuti Khristu adzakhala nafe wamoyo nthawi zonse m'mitima mwathu.

5. CHISANGALALO CHA MWAYI WACHIWIRI

Munthu wotchedwa Harold Hughes analandira maulemu ambiri mu ntchito yake yolemekezeka ngati wamkuru wakunyumba yamalamulo ku America, koma ulemu womwe udaposa onse kwa iye ndi umene analandira atangodzipereka kwa Yesu.

Harold ankawerenga ndi kuphunzira mau a Mulungu M'baibulo yekha m'chipinda chake usiku wina pamene anamva kukhudza pa bondo la mkono wake. Atatukula nkhopre anaona kuti ndi ana ake a akazi awiri aang'ono, ataima mwachete pafupi naye atavala zovala zavo zogonera. Anawayang'ana iwo kwa kanthawi, anali osinthika kwambiri, ndipo anali atasowana nawo kwa nthawi yaitali chifukwa chamoyo wake wauchidakwa.



Ndiye mwana wamn'gono kwambiri, Carol, anati: "Adadi, tabwera kudzakupsopsonani kuti mugone bwino." Maso abamboyu adachita mdima. Panali patapita nthawi yaitali kuyambira pamene anatsirizira kupsopsonana nawo ana ake. Koma panopa anawanso sanaonetse mantha, anabwera m'maso mwawo mokongola ndi moyera. Bambo anabwera kunyumba tsopano.

Yesu anatipatsadi ife anthu mwayi wachiwiri. Iye amachotsa milandu yonse yochotsa chiyembekezo ndi kutitengera kuyambanso kwatsopano.

Mpulumutsi akufuna wina ali yense wa lye abwerere kunyumba. Kodi mwavomera kuitana kwachikondi kwa Khristuku? Kulandira kukhululukidwa ndi kuyeretsedwa ndi Mulungu ndikosavuta ndi kwakuya ngati kungotambasula mikono yanu kuti mwana wanu akukhumbatireni, kukupsopsonani.

Ngati simunakhulupilirebe mwa Khristu ngati Mpulumutsi wanu, mutha kutero nthawi inoyi pongopemphera motere:

"Atate, ndiri ndi chisoni ndi moyo wanga wakale wauchimo. Zikomo putuma mwana wanu Yesu Khristu ku dziko lino lapansi kudzafa m'malo mwa ine. Yesu, chonde, mundikhulukire machimo anga ndipo mudze mukhale m'moyo wanga ndikundipulumutsa. Ndifuna mwayi wachiwiri pa moyo wanga - ndikufuna kubadwanso mwatsopano. Koposa zonse, ndifuna ndikhale pa ubale nanu tsiku ndi tsiku. Zikomo chifukwa chochita chozizwa ichi kwa ine. M'dzina la Yesu Khristu, Amen."

Pangani kufufuza kozizwitsa uku: Ife tikakonzekera kubwera, lye amachita mbali yakupulumutsa.

M'MENE TIMALANDILIRA MOYO WATSOPANO KUCHOKERA KWA KRISTU

- (i) Timakhulipilira mwa lye ndi kumulandira lye ngati Mpulumutsi ndi ambuye.
- (ii) Timakhazikitsa ubale ndi lye. (Nthawi zonse kukhala ndi pemphero ndi maphunziro a Mawu ake ndizofunika kwambiri).
- (iii) Khristu amagwira ntchito mwa Mzimu wake woyerwa kubweretsa makhalidwe ake abwino kuti alowe m'malo mwa makhalidwe athu oipa omwe amawachotsa.

ZA TSOGOLO LANU

Madotolo awa, Patricia ndi David Mrazeki anaona zoswetsa mtima zambiri mu ntchito yawo. Monga wotswirika pa nkhani ya matenda a ana, anachita ndi ana ambiri ovutika. Koma anazizwa poona kuti ana ena amachira pamene ena amapsinjika ndi mavuto amodzimodzi omwewo. Chifukwa chiyani? ndichifukwa chiyani ana ena mwachitsanzo, amamwa mankhwala osokoneza bongo pamene wina apita ku sukulu ya ukachenjede? Nanga bwanji ana ena ozunzidwa amakula nkudzakhalanso ozunza anzawo, pamene ena amadzakhala makolo abwino?

A Mrazeki awa anapanga kafukufuku wakuya kuti apeze mayankho a mafunsowa. Mu ku phunzira kwao khalidwe lina limapezeka mwa anawa omwe anadutsa muzoopsa zomwe anakumanapo nazo, koma nakhala ndi moyo wabwino ndi wathanzi. Chinsinsi chake chinali chiyani? "Mayang'anidwe abwino a moyo ndichiyembekezo."

Chiyembekezo chinabweretsa kusintha. Chiyembekezo, koposa zonse, chimathandiza ife kumenyana ndi kugonjetsa zovuta zomwe zakhala zikuzunza m'miyoyo yathu.

Anthu amafunitsitsa chiyembekezo. Koma nanga timachipeza bwanji? Chiyembekezo ndichovuta kuchipeza m'dziko lathu lapansili mpaka titayang'ana molunjika ku bukhu lopatulika ndi maulosi ake. Phunziro ili likutithandizanso kufufuza ulosi wopatsa chidwi umene watakasa anthu ambiri ndi chiyembekezo chakuya.

1. ULOSI WOZIWITSA WA MU BAIBULO

Pafupifupi zaka mazana asanu asanabadwe Yesu Khristu, Mulungu anaonetsera za tsogolo la dziko kupyolera mwa mneneri Daniel.

Mulungu anaperekeratu ndondomeko ya mbiri ya dziko lapansi ya zaka zikwi ziwiri mazana asanu zamtsogolo, kuyambira mu nthawi ya Danieli mpaka nthawi yathu ino.

Ulosi uwu unachokera mu loto la mfumu Nebukadinezara, wa dziko la Babulo zaka zikwi ziwiri mazana asanu zapitazo. Lotoli linazunza mfumuyu koma sanathenso kulikumbukira ngakhale atadzuka! Anzeru onse a ku Babulo atalephera kuthandiza kumukumbutsa mfumuyu loto lake kuti limasuliridwe, Mu Heberi wang'ono wogwidwa ukapolo dzina lake Daniel anaonekera akulengeza kuti Mulungu wakumwamba angathe kuvumbuuitsa zinsinsi zonse.



Ataima pamaso pa mfumu, Daniel molimba mtima ananena! "Inu mfumu munapenya ndi kuona FANO LALIKURU Fanoli linali lalikuru, ndi kunezemira kwache kunaposa; linali kuima popenyana ndi inu, ndi maonekedwe ache anali oposa. Fano ili tsono, mutu wache unali wagolidi wabwino, chifukwa chache ndi manja ache zasiliva, mimba yache ndi chiuno chache zamkuwa, miyendo yache yachitsulo, mapaziache mwina chitsulo mwina dongo. Munali chipenyere kufikira mwala unasemedwa popanda manja, umene unagunda fanoli pa mapaziache okhala chitsulo ndi dongo."

"Pamenepo chitsulo, dongo, mkuwa, siliva, ndi golidi, zinapereka pamodzi, nizisanduka ngati nungu wa pa madwale a malimwe; ndi mphepo inaziluza osapezekanso malo awo; ndi MWALA UDAGUNDA DZIKO LONSE LAPANSI." - Daniel 2:31-35.

Fano ili, poliona koyamba, lingathe kuoneka ngati liribe zambiri zokhudzana ndi chiyembekezo cha moyo wathu mu nthawi yathuyi koma khalani cheru muone.

2. ULOSI UMASULIRIDWA

Atatha kunena mwazonse zomwe analota mfumuzo mopanda kuchotsa kapena kuonjezera, mneneri Daniel analongosola motere:

"Ili ndi loto; kumasulira kwache tsono tikufotokozerani mfumu." - Daniel 2:36.

MUTU WA GOLIDI:

Kodi ndi ufumu uti wa dziko womwe Daniel adauza mfumu kuti ukuimiliridwa ndi mutu wa golidi.

"Inu mfumu ndinu mfumu ya mafumu, pakuti Mulungu wakumwamba anakupatsani ufumu, ndi mphamvu yaikuri, ndi ulemu... INU NDINU MUTUWO WAGOLIDI." - Daniel 2:37, 38.



Daniel amuuza wolamulira wa dziko dera lalikulu kwambiri ndi lamphamu pa dziko lonse lapansi. "Nebukadinezara, Mulungu akukuuzani kuti ufumu wanuwa wa Babulo ukufanizidwa ndi mutu wa Golidi wafanolo".

CHIFUWA NDI MANJA ZA SILIVA

Mukuona kwa umunthu, zinali kuoneka kuti Babulo adzalamulira nthawi zonse. Koma kodi ulosi ukunena kuti chidzachitika ndi chiyani pambuyo pake?



"Ndipambuyo pa inu padzauka ufumu wina wochepta ndi wanu." - Daniel 2:39.

Pokwanirtsa ulosi wa Mulunguwu, ufumu wa Nebukadinezara unagonjetsedwa ndi ufumu wa a Medi ndi Apelezi motsogozedwa ndi mfumu Sairasi m'chaka cha 539 B.C. Choncho chifuwa ndi manja zasiliva zikuimira a Medi ndi a Perezi, ufumu winanso wamphamvu.



MIMBA NDI CHIUNO ZA MKUWA

Kodi mbali imeneyi ikuimira chiyani pa chifano chachikuluchi?

"Ndi ufumu wina wachitatu wamkuwa wakuchita ufumu pa dziko lonse lapansi." - Daniel 2:39.

Mimba ndi chiuno zamkuwa zimaimira ufumu wa Chihelene womwe motsogozedwa ndi Alexander, anagonjetsa a Medi ndi a Perezi, kusandulika ufumu waukulu wachitatu padziklo lonse lapansi womwe unalamulira kuyambira m'chaka cha 331 mpaka 168 BC.



MIYENDO YA CHITSULO

"Ndi ufumu wachinayi (anatero mneneri) udzakhala ngati chitsulo, popeza chitsulo chiphwanya ndi kufooketsa zonse; ndipo monga chitsulo chiswa zonsezi, uwu udzaphwanya ndi kuswa." - Daniel 2:40.

Atafa Alexander, ufumu wake unafooka ndikugawika m'magulu odana mpaka pamene, m'chaka cha 168 BC, pa nkhondo ya ku Pydna, "ufumu wa chitsulo" wa Roma una phwanya Ahelene.

Augustus Caesar (Kaisala) anali kulamulira ufumu wa boma pamene Yesu anabadwa pafupifupi zaka zikwi ziwiri zapitazo (Luka 2:1). Khristu ndi atumwi ake anakhala munthawi imeneyi ya ulamuliro woyimiridwa ndi miyendo ya chitsulo. Gibbon, wolemba wa mbiri yakale wa mu zaka za m'mazana khumi ndi asanu ndi mphambu zitatu (18th Century), analemba za nthawi imeneyi, popanda kukaika anali ndi ulosi Daniel mmaganizo pamene analemba kuti "Zifanizo za golidi, kapena siliva, kapena mkuwa, zomwe zimathandizira kuimirira maiko ndi mafumu awo, anaphwanyidwadi ndi ufumu wa chitsulo wa Roma. Edward Gibbon. Mbiri ya kugwa ndi kudzukanso kwa ufumu wa Roma, tsamba 89, vol. 4 (*John D. Morris and company*).

Taganizirani inu kwa kamphindi za ulosiwu mwa umunthu Daniel akanatha bwanji kukhala ndi m'ndandanda wa maufumu anayi akutsogolo molondola pamene iye anali kukhala munthawi ya ufumu woyambirirawo wa Baibulo? Tiri ndi vuto lodziwa za momwe malonda akhalire Sabata yamawa! Koma Babulo, Medi ndi Perezi, Aherene, ndi Roma anakhaladi maufumu otsatana kulamulira monga mmene ulosi unaliri ngati ana omvera a sukulu pamzere.

Kodi Mulungu akulamulira pa za mtsogolo? Tingakhale ndi chiyembekezo pa chikonzero chake? Yankho ndi loti, "Eya."

MAPAZI NDI ZALA ZA DONGO KUSAKANIZANA NDI CHITSULO

Kodi ufumu wachisanu udzabwera pambuyo pa ufumuwu wa Roma?



"Ndipo umo mudaonera mapazi ndi zala zache, mwina dongo la woumba, mwina chitsulo, UFUMUWU UDZAKHALA WOGAWANIKANA; Koma momwemo mudzakhala mphamvu ya chitsulo; popeza mudaona chitsulo cosanganizika ndi dongo ndi zala za mapazi, mwina chitsulo ndi mwina dongo, momwemo ufumuwo mwina wolimba mwina wogamphuka." - Daniel 2:41, 42.

Mneneri analosera, osati ufumu wachisanu wa dziko, koma kugawikana kwa ufumu wa chitsulo wa Roma. Roma ayenera kuthyoka nkupangika timaufumu tina khumi ting'onuting'ono, tomwe tiimiridwa ndi mapazi ndi zala za kumapazi za chifanocho.

Kodi izi zidachitikadi? Inde zinachitika. Mu zaka za zana lachinayi ndi la chisanu za mbiri ya Chikhristu, anthu ankhanza ochokera ku mpoto anadzasokaneza Roma yemwe anataya mphamvu yake, namugonjetsa pompatsa mavuto ndi nkhondo yomugonjetsa pafupi pafupi. Posakhalitsa Madera khumi amitundu ya mu ufumuwo anapeza nawo ulamuliro wa mbali zina za kumadzulo kwa Roma, ndi maboma khumi anakhala odziimira paokha mmalire a Ulaya. Izi ndizo zimene zala khumi zikuimirira, maiko atsopano khumi a ku Ulaya lero.

3. TSIKU LATHU MU ULOSI

Kodi ulosi wa Danieli ukuonetsa kuti kuyesa kudzachitika masiku athu ano mu ulosi kogwiranitsa maiko a ku ulayawa pansi pa mtsogoleri mmodzi?

"Ndi umo mudaonera chitsulo chosanganiza ndi dongo, iwo adzadzisokoneza ndi ana a anthu wamba; koma SADZAPHATIKIZANA, monga umo chitsulo sichimasanganizika ndi dongo." - Daniel 2:43.

Nthawi ndi nthawi, amuna amphanvu ayesetsa kugwiranitsa maiko a ku Ulaya, koma nthawi zonzezi alephera. Napolionyi anakhala ngati angathe kuposa ena onse, koma mwina poganzira za ulosiwu,



pomwe ankathawa atagonjetsedwa ku nkhondo ya ku Waterloo, analira, "Mulungu wamphamvu zonse wandikulira."

Kaiser Wilhelm wachiwiri ndi Adolf Hitler anadza ndimagulu ankhondo oopsa ndi amphanmu kwambiri pa nthawi yawo. Koma aliyense analephera kugwirizanitsa maiko a ku Ulaya pansi pa utsogoleri wawo. Nanga ndi chifukwa chiyani? Ndichifukwa choti mawu a Mulungu anali kukwaniritsidwa. "Anthu adzasanganikira ndipo sadzagwirizanitsika." Zotsatira zake za nkhondo zonse ziwiri za dziko lonse lapansi zotsimikizira kuti Mulungu amagwiriziza tsogolo la dziko lapansi m'dzanja lake; lye ndiye amene akulamulira zonse. Izi ndi zokwana kutipatsa ife chiyembekezo, mtendere wa mumtima, ndi kulimba mtima mu chikonzero chake pa miyoyo yathu.

4. KUONANSO ZA KUTSOGOLO

Mbali imodzi yokha ya ulosi wa Daniel ndi yomwe siinakwaniritsidwe. Kodi tanthauzo la mwala umene ukuphwanya fanoli kumapazi, napela fanolo, nusandulika phiri lalikulo lodzaza pa dziko lonse, ndi chiyani?

"NDIPO MASIKU A MAFUMU AJA (MAIKO ATSOPANO AKU ULAYA), MULUNGU WA KUMWAMBA ADZAIKA UFUMU woti sudzaonongeka ku nthawi zonse, ndi ulamuliro wace sudzasiyidwira mtundu wina wa anthu, koma udzaphwanya ndi kutha maufumu ao onse. NDIDZAKHALA CHIKHALIRE." - Daniel 2:44.

"Mafumu aja" angalozere maufumu okhawo a mapazi ndi zala za fanolo - Atsogoleri a maiko atsopano a ku ulaya, kulozera kunthawi yathu ino ya lero. Mwala umene unapangidwa wopanda manja uli kufuna kuphwanya fano ndi kuliswa kulipera, ndipo iwo udzadzaza dziko lonse lapansi (ndime ya 34, 35, 45). Posachedwa Yesu atsika kuchokera kumwamba "Kudzakhazikitsa Ufumu," Ufumu wake wa chisangalalo ndi mtendere. Pomwepo, Khristu, thanthwe la mibadwo ndi mfumu ya mafumu, adzalamulira dziko lapansi kwa tuyaya!

Chirichonse cha mu ulosi wa Daniel 2 chachitika kupatulapo mwalawu kuphwanya fanoli. Mchikonzero cha nthawi ya Mulungu, tatsala pang'ono kufika pa mapeto penipeni, kuti Yesu abwere padziko lapansi. Yesu Khristu, Mwana wa Mulungu, ali pafupi kutsiriza kulimbana kwamwazi komwe kwatenga nthawi yaitali mu mbiri ya munthu ndi kudzakhazikitsa ufumu wosatha wa chikondi ndi chisomo.

5. LOTO LA MFUMU NDI INU

Ulosi uwu ukuulula dzanja lotsogolera la Mulungu mu nthawi ya kudza ndi kugwa kwa mafuko. Mulungu amadziwa zammbuyo, ndipo ulosi uwu wa m'Baibulo ukuonetsera poyer a kuti lye akudziwanso zam'tsogolo.

Ngati Mulungu amatsogolera mmene maufumu akuyendera mwandondomeko yotereyi, ndithudi, atha kutsogolera moyo uliwonsse. Yesu anatitsimikizira ife: "Ngakhale tsitsi la mmutu mwanu liwerengedwa ndi ine. Chotero musaope" (Mateyu 10:30-31).



Mphatso ya Mulungu ya chikhulupiro itha kukhala mankhwala a mavuto, madandaulo ndi mantha athu. Chiyembekezo chomwe amachitakasa chitha kukhala mzati wa mitima yathu (Ahebri 6:19).

Wophunzira wa mzaka zamazana khumi mphambu zisanu ndi limodzi (16th Century), Erasmus analongosola zomwe zinachitika pa ulendo wa panyanja zomwe sadaziiwale moyo wake wonse. Sitima yake inavutika ndi kuonongeka ndi mafunde. Pamene mafunde a ukali anamenya pa Sitima yake niyamba kuphwanyika, ngakhale oyendetsa sitimayo anaopa okwera nawo anali pafupi kuyamba

kukomoka Ena nafuula kufuna chithandizo kwa owayendetsa, poimba nyimbo zotamanda za uzimu, ndi kupemphera mofuula.



Erasmus anaona munthu mmodzi woyenda nawo m'sitimayo, yemwe anachita mosiyana ndi ena onse. "Mwa ife tonse," Erasmus analemba, "mmodzi yemwe sanaonetse kugwedezeza anali mkazi wachisungwana yemwe anali ndi mwana yemwe amamusamalira. Ndiyekhayo yemwe sanafuule nefe, kapena kulira, kapena kukambirana ndi kumwamba. Sanachite kena kalikonse koma kupemphera mwachete kwa iye yekha uku akumugwira mwana wake momufungata pa chifuwa pake."

Pemphero iri, Erasmus anazindikira, kuti linali kupitiriza mapemphero omwe mayiyu anali kuchita nthawi zonse m'moyo wake. Anaonetsa wodzipereka mwa iye yekha kwa Mulungu.

M'mene Sitima inayamba kumira, msungwanayu anaikidwa pa thabwa, atapatsidwa chopalasira kuti agwirits ntchito, natengedwa ndi mafundewo. Anamgwiritsabe mwana wake ndi dzanja limodzi ndi kusambira ndi dzanja linali. Ndi anthu ochepta omwe anaganiza kuti msungwanayu apulumuka ku mafunde woopsawo.

Koma chikhulupiro chake ndi kusagwedezeza kwake kunampanga kuhala tcheru. Iye ndi mwana wake ndiwo adali oyamba kufika ku gombe.

Chiyembekezo mwa Mulungu wodalirikayo chingabweretse kusintha konse ngakhale pamene dziko likuoneka ngati likuphwasuka motizungulira. Sitiri tokha kupalasa ngalawa ayi, pali dzanja lamphamu likutitsoglera ndi kutigwira dzanja.

Mukabwera kwa Yesu athunthu modzipereka adzakupatsani chikhulupiro
chimene chidzakudutsitsani m'mafunde. Pezani inu mtendere
wodabwitsawu umene Yesu amalonjeza.

**"Mtendere ndikusiyirani inu, mtendere wanga ndikupatsani inu...
Mtimu wanu usabvutike, kapena usacite mantha." - Yohane 14:27.**

Kodi muli ndi mtendere umenewu? Ngati ndi choncho, thokozani Yesu Mpulumutsi wanu. Ngati sichoncho, bwanji osamuitana iye m'moyo wanu lero?



YESU AKADZABWERERA INU

Patatha zaka zambiri zankhanza, Armando Vallades anaonda, kungokhala ngati chithunzi cha momwe analiri kale. Amagwira ukaidi wa zaka makumi atatu mu imodzi ya ndende za Castro chifukwa chopezeka akupemphera m'chalichi pa tsiku la Khrismasi. Oyang'anira ndende anamukhazika ndi njala, kumuzunza ndi kumunyoza komabe sanalole kusiya chikhulupiriro chake.

China chake chinampanga iye kupidabe chitsogolo: Ionjezo lomwe anapanga kwa msungwana wina wotchedwa Martha. Anakomana nafunsirana ubwenzi iye adakali m'ndende. Msungwanayu anakhudzidwa kwambiri ndi chikhulupiriro cha Armadochi. Atakwatitsidwa m'ndende momwemo pa mwambo womwe unachitikira mchipinda china momwemo, Martha anakakamizika kupita ku Miami.

Kulekana kwavo kunali kowawa. Koma Armando anayesetsa kumulonjeza wokondedwa wake polemba, pakapepala kosaoneka bwino kotayidwa pomwe analembapo lonjezano lake lakuti: "Ndidzabwera kwa iwe, ngakhale mavuto adzachulike sindidzawasamala ayi."

Wam'hdendeyu anatsimikiza kuti tsiku lina iye ndi Martha adzapanga malumbiro awa a ukwati mu kachisi wa Mulungu pamaso pa Mulungu. Tsiku lina kulumikizana kwavo kudzakhala kwathunthu. "Uli ndi ine nthawi zonse." Anamuza choncho msungwanayo.

Lonjezoli, zinapangitsa Armando kupidirirabe chitsogolo kupyola zaka zonse zozunzidwa zidakampangitsa munthu aliyense kutaya mzimu wake. Ndipo zinampangitsa Martha kupita chitsogolo. Anayesetsa kuwadziwitsa anthu poyer a mosatopa zacholinga cha mwamuna wake. Sanataye chiyembekezo chake.

1. LONJEZANO

Nthawi zina ungayesedwe kuzizwa kuti kodi Khristu adzatsikadi tsiku lina kuchoka kumwambaku kudzalumikizanano nefe? Modabwitsa talekanitsidwa ndi lye kwa nthawi yaitali tsopano. Kathedwe kabwino kotere mbiri yaitali, yoopsa ya dziko lapansi kudzaoneka yabwino kwambiri kukhala yoona. Koma pali chinthu chimodzi chomwe chingasunge chikhulupiriro chathu kukhalabe chamoyo m'mitima yathu. Ichi ndicho lonjezano lake la Yesu kuti adzabweranso. Yesu asanachoke kwa ophunzira ake kupita kumwamba, anawalonjeza.

"Mtima wanu usabvutike, mukhulupirira Mulungu, Khulupirirani inenso. M'nyumba ya Atate wanga alimo malo okhalamo ambiri. Ngati sikudali koteri ndikadakuuzani inu; pakuti ndipita kukakukonzerani inu malo, ndipo ngati ndipita kukakukonzerani inu malo NDIDZABWERANSO, ndipo ndidzalandira inu kwa ine ndekha; kuti kumene kuli ineko, mukakhale inunso." - 1 Yohane 14:1-3.

Yesu asanakwere kunka kumwamba, anawatsimikizira ophunzira ake, 'Ndidzabweranso!' anawalonjeza kudzawatenga onse omukhulupirira iye kunka nawo ku malo apadera omwe watikonzera. Mawu a Mulungu akunena za kubwera kwake kwa chiwiri pafupifupi nthawi zikwi ziwiri mazana asanu (2,500 times). Nkhani yoti Yesu akubweranso kachiwiri ku dziko lapansi ndi yoona ngati momwe anakhaliradi padzikio lapansi zaka zikwi ziwiri zapitazo.



M'mbuyomo Mulungu analonjeza za kudza kwa Mesiya, wotimasula yemwe akadadzitengera pa lye yekha mphulupulu machimo athu ndikutipatsa chikhululukiro cha tchimo la anthu. Lonjezolo lidaoneka labwino kulikhulupirira kwa anthu ambiri m'nthawi yakaleyo omwe anavutika m'moyo wawo. Koma Yesu anabweradi nafa pa mtanda.

Lonjezano lija linakwaniritsidwa mokondweretsa koposa momwe anthu amaganizira. Lonjezo lake lakubweranso lidzakwaniritsidwa. Tingathe kudalira pa lye wotikondayo, kuti adzabwera ndi kusonkhanitsa iwo womwe lye adawalipirira mtengo wapatali .

Kupyolera mu undende wake wonse, Armando anapitirira kulemba ndakatulo, mauthenga ndi zojambula kwa Martha mozembetsa. Ndipo msungwanayu anazisindikizitsa zolembadwazi. Luso ndi uthenga wa zolembadwazi zinachititsa chidwi padziko.

Maboma anayamba kuumiriza Castro kuti atulutse andende achikumbumtima. Purezidenti wa Faransa analowereraponso ndipo pamapeto pake m;chaka cha 1982 Armando anatulutsidwa natumizidwa ku Parisi pa ndege. Zinamuvuta kukhulupirira kuti ali mfulu tsopano ngakhale pamene ndege yomwe anakwera inatera. Koma tsopano patatha zaka makumi awiri akuzunzika, ndi kudikirira,ndi kukhumba, Amarndo anathamangira napezekanso m'manja a Martha.

Patapita miyezi yochepa, anthu awiriwa ali wokondwa anaima pamaso pa mpingo wa St Kiera ku Miami kupanga malumbiro awo a ukwati. Kulunzanitsidwa kwavo kunatheka tsopano. Lonjezano linakwaniritsidwa. "Ndidzabweranso kwa iwe."

Kodi mungathe inu kuganizira chisangalalo chomwe chidzakhale panthawiyi yolumikizanayi pamene tidzamuona Yesu Khristu wathu maso ndi maso? Kuonekera kwake kwa ulemerero kudzakwirira zisoni ndi zokhumudwitsa zathu zonse, kudzapukuta zowawa zomwe zakhala zobisika m'mitima yathu. Kubweranso kwa Yesu kudzakwaniritsa khumbo lathu ndi chiyembekezo chathu cha pansi pa mtima. Ndipo tidzakhala pa mgwirizano wosatha ndi munthu woziwitsa wa dziko lonse. Yesu akubwera posachedwa! Kodi inu mukufunitsitsa kudzakomana naye?

2. YESU ADZABWERA BWANJI



(1) Kodi Yesu adzabwera mwa chinsinsi?

"Onani, Ine (Yesu) ndakuuziranitu pasadafike. Chifukwa chache akanena kwa inu, onani iye ali m'chipululu; musamukeko. Onani ali m'zipinda musabvomereze, pakuti monga mphezi idzera ku m'mawa nionekera kufikira kumadzulo; KOTERO KUDZAKHALA KUFIKA KWACE KWA MWANA WA MUNTHU." - Mateyu 24:25-27.

Kung'anima kwa mphezi kumawala moonekeratu patali, koteronso kudzakhala kudza kwa Yesu, osati mwachinsinsi ayi, kapena chooneka malo amodzi.

(2) Kodi Yesu adzabweranso ngati munthu weniweni?

"Ndipo pakukhala iwo (Ophunzira a Yesu) chipenyere kumwamba pomuka lye, taonani amuna awiri obvala zoyerwa anaimirira pambali pao; amenenso anati. Amuna a ku Galileya, muimiranji ndi kuyang'ana kumwamba? YESU AMENE WALANDRIDWA KUNKA KUMWAMBA kuchokera kwa inu ADZADZA momwemo monga MUNAMUONA ALI KUPITA KUMWAMBA." - Machitidwe 1:10-11.

Patsiku lake lonyamuka kuchoka pa dziko lathuli angelo anawatsimikizira ophunzira kuti, "Yesu yemweyo" watengedwa kukwera kumwamba osati wina ayi - adzabweranso yekha ngati mfumu ya mafumu. Yesu yemwe anachiritsa odwala ndi kupenyetsa akhungu. Yesu yemweyo adalankhula mofatsa kwa mayi wogwidwa m'chigololo. Yesu yemweyo yemwe adapukuta misozi ya wolira nalandira ana

m'chifukato chake. Yesu yemwe adafa pa mtanda wa Karavali, napuma m'manda naukanso kwa akufa pa tsiku lachitatu.

(3) Kodi Yesu adzabwera moti tidzamuona?

**"Taonani adza ndi mitambo, ndipo DISO LIRILONSE LIDZAMPENYA IYE." - Chibvumbulutso 1:7
(mbali yoyamba).**

Onse amoyo pamene Yesu adzabweranso, olungama ndi ochimwa omwe pamodzi, adzachitira umboni kudza kwake. Kodi Yesu adanena kuti ndi anthu angati omwe adzaone kudza kwake?

"Ndipo pomwepo padzaoneka m'thambo chizindikiro cha mwana wa munthu; ndipo mitundu yonse ya padziko lapansi idzadziguguda pa chifuwa, nidzapenya mwana wa munthu alinkudza pa mitambo ya kumwamba, ndi mphamvu ndi ulemelero waukuru." - Mateyu 24:30.

Munthu aliyense, munthu wamoyo padziko lathuli lapansi adzaona Yesu akubweranso.

(4) Kodi omwe adzabwere naye Yesu pamodzi ndani?

"Koma pamene mwana wa munthu adzadza mu ulemelero wache, ndi Angelo onse pamodzi naye, pomwepo iye adzakhala pachimpando cha kuwala kwache." - Mateyu 25:31.

Tangoganizirani inu m'mene zidzakhalire Yesu akamadzabweranso mu ulemerero wake atazunguliridwa ndi "Angelo Onse."



(5) Tingathe ife kuneneratu nthawi yeniyeni yomwe Yesu adzabwerere?

"Koma za tsiku ilo ndi nthawi yache sadziwa munthu aliyense, angakhale Angelo a Kumwamba, kapena mwana, Koma Atate yekha... Chifukwa chache khalani inunso okonzekeratu; chifukwa munthawi m'mene simuganizira, mwana wa munthu adzadza." - Mateyu 24:36, 44.

Aliyense adzaona Yesu ndi kufika kwake kwa ulemelero. Koma ambiri adzakhala asanakonzekere. Inu mwakonzekera panokha kuti Yesu abwere?

3. KODI YESU ADZACHITA CHIYANI AKADZABWERANSO

(1) Yesu adzasonkhanitsa opulumutsidwa (osankhika) onse Pamodzi.

"Ndipo iye adzatumiza Angelo ache ndi kulira kwakukuru kwa lipenga, ndipo iwo adzasonkhanitsa osankhidwa ache ku mphepo zinai, kuyambira malekezero a thambo kufikira malekezero ache ena." - Mateyu 24:31.

Ngati mwalola Yesu kukonza mumtima mwanu ndi m'moyo mwanu, mudzamupatsa moni wachimwemwe ngati Mpulumutsi wanu.

(2) Yesu adzaukitsa akufa olungama.

"Pakuti Ambuye adzatsika kumwamba mwini yekha ndi mpfuu, ndi mawu a M'ngelo wamkuru, ndi lipenga la Mulungu, ndipo AKUFA MWA AMBUYE ADZAYAMBA KUUKA." - 1 Atesalonika 4:16.

Yesu adzatsika kumwamba ndi mpfuu. Liu lake lamphamvu limveka dziko lonse. Nilitsegula manda ndi kuukitsa miyanda ya anthu omwe anamulandira mmibadwo yonse. Tsikutu lalikuru nanga limeneli.

(3) Yesu adzasintha oyera onse pakubweranso kwake - osati akufa olungama okha ayi, koma ngakhalenso olungama amoyo.

"Pamenepo ife okhala ndi moyo, otsalafe, tidzakwatulidwa nao pamodzi m'mitambo kukakomana ndi Ambuye mumlengalenga, ndipo potero tidzakhala ndi Ambuye nthawi zonse." - 1 Atesalonika 4:17.

Potikonzetsera ife moyo tuyaya, Yesu akusintha matupi athu a kufawa kuwapanga okongola ndi wosafa.



"Taonani ndikuuzani chinsinsi; sitidzagona tonse, koma tonse tidzasandulika, m'kamphindi, m'kuthwanima kwa diso, pa LIPENGA LOTSIRIZA; ndipo ife TIDZASANDULIKA. Pakuti chovunda ichi chiyenera kuvala chisavundi, ndi cha imfa ichi kuvala chosafa." - 1 Akorinto 15:51-53.

Yesu podzabwera tonse tidzasinthika. Tangoganizani kopandanso kufa ziwalo, kopanda matenda. Zipatala kutsekedwa ndi malo osungira maliro kutsekedwa. Khristu wabwera!

(4) Yesu adzatenga olungama onse kupita nawo Kumwamba. Yesu mwini analonjeza kuti, "Ndidzabweranso kudzatenga inu kuti mukakhale nane." M'nyumba ya Atate wanga (Yohane 14:1-3). Petro akunena za cholandira cha opulumutsidwa "chomwe chasungidwira inu kumwamba" (1 Petro 1:4). Tikuyembekeza kudzaona zodabwitsa za mzinda wa Mulungu, Yerusalem watsopano, ndi kufika pomdziwa Atate wathu wakumwamba.

(5) Yesu adzathetsa choipa ndi masautso onse kunthawi zonse.

Ochimwa omwe adakhala akukana chisomo chomwe Yesu anapereka adziweruza okha. Poona nkhopo ya Yesu ikutsikira kwa iwo kuchokera m'mitambo, adzazindikira machimo awo namva kuwawa kovuta kukupirira, nadzalira kwa mapiri ndi matanthwe, "Tigwereni ife ndi kutibisa ku nkhopo ya lye amene akhala pa pampando wa Chifumu ndi ku mkwiyo wa Mwana Wankhosa!" (Chibvumbulutso 6:16). Adzafuna imfa koposa kuonana ndi nkhopo ya Yesu yowayang'a mosalekeza.

Akudziwa kuti mawu amene akufuula ndi omwe aja adawaitana iwo nthawi ina kuti alandira chisomo chake. Iwo amene adaziipsa ndi chuma ndi zokondweretsa za moyo, kapena maudindo tsopano adziwa kuti anakana chinthu chokhacho chopambana m'moyo.

Ndi chibvumbulutso chopweteka. Komatu palibe ndi mmodzi yemwe anayenera kutaika. Mulungu mwini "Sakondwera nayo imfa ya ochimwa" (Ezakiel 33:11). Iye, safuna kuti wina akaonongeke, koma kuti adze ku kulapa (2 Petro 3:9). Yesu akutidandaulira ife, "Idzani kuno inu nonse akulema ndi akuthodwa, ndipo ndidzakupumulitsani" (Mateyu 11:28). Koma chodabwitsa ndi chomvetsa chisoni, ena amakana kuitanira kwake kwa chisomo.

4. KODI INU MWAKONZEKA PAKUBWERA YESU

Zinamutengera Yesu mtengo waukulu kutipatsa ife tsogolo la ulemelero ndi iye. "M'nyumba ya Atate anga." Zinamutengera moyo wake!

"Kotero KHRISTUNSO ATAPEREKEDWA NSEMBE KAMODZI, ku kasenza machimo a anthu ambiri, adzaonekera pa nthawi yachiwiri, wopanda uchimo, kwa iwo amene amulandira kufikira chipulumutso." - Ahebri 9:28.

Mpulunutsi yemwe anafa pa mtanda kuchotsa machimo ako adzaonekera kachiwiri ndipo adzabweretsa chipulumutso kwa iwo omwe akumuyembekezera. Yesu anadziperek yekha nsembe ndicholinga chotipatsa aliyense wa ife chipulumutso. Koma popanda kubweranso kachiwiri, ntchito ya mtanda ikanakhala



yopanda pake. Khristu akufuna kutipatsa ife kwathu kwamuyaya ndi kotetezedwa ndi lye, kuti izi zitheke, tiyenera ife kumulola lye kulamulira mitima yathu ngati mpulumutsi ndi Ambuye kuyambira tsopano.

M'mawa wa pa August 16, 1945, mwana wina wam'ngono anathamanga kudutsa nyumba za a Shantung kumpoto kwa dziko la China akufuula kuti waona ndege mlengalenga. Onse amene anali ndi mphamvu pa mudzipo anatuluka panja nayang'ana kumwamba. Anthuwatu anali atakhala zaka zambiri mosalidwa, kukanidwa ndi kumanidwa, ndi chikhumbokhumbo, andende omwe anasungidwa ndi dziko la Japani ngati akaidi am'maiko odana nawo.

Kwambiri chinthu chimodzi chokha, chomwe chinawapanga kukhalabe amoyo muuzimu, ndicho chiyembekezo chakuti tsiku lina nkondoyi idzatha.

Nyesi ya magetsi inawadutsa gulu la anthu chikwi ndi mazana asanu am'ndende omwe anali ndi moyobe. Pamene anazindikira kuti nkutheka ndegeyo imadzera iwo. Pamene phokoso la ndegeyo linakulirakulirabe, wina wa iwo anafulula, "TAONANI, pandegeyo pali mbendera ya dziko la AMERIKA! Yopetedwa mmbali mwake akutikwezel a mikono Akutidziwa, akubwera kudzatitenga."



Panthawiyi chisangalalo chimakulirakulirabe koposa mwa anthu ovutika ofooka, ofuna kwavo wa. Chisokane kero chachikuru chinabuka. Anthu ankathamanga mutimagulu mozungulira, akufuula mokweza ndi manja awo m'mwamba ndi kulira.

Mwadzidzidzi kunagwa bata pa gululi pamene onse anapenya kensi kwa ndegeyi kukutseguka ndipo anthu akutsika mundegeyo pogwiritsa ntchito matumba otsikira ndege idakali m'mwamba aja. Owapulumutsa awo samangobwera kokha tsiku lina ayi, amabwera lero, PANOPA kuti akhale pakati pawo.

Gululi linakhamukira kuchipata cha mudziwo. Palibe anaganiziranso za mfuti zoopsa zomwe zinawaloza kuchokera pa chinyumba chachitali cha owayang'anila ayi. Atakhala zaka zambiri zogwetsedwa mphwayi, kusowa abwenzi, anaswa chipatacho nathamangira komwe owapulumutsawa amatera.

Posakhalitsa anthuwa anatembenuka nallowanso mmudziwo atawanyamula asirikali owapulumutsa aja. Wolamulira ku malo awa anawapereka iwo wopanda nkondo. Nkhondo inathadi. Ufulu unabwera. Dziko linakhalanso latsopano zedi.

Posachedwa Mulungu wathu, nthano yaitali yoopsa ya munthu Mpulumutsi wathu, adzatsika kuchokera m'mitambo kudzatipulumutsa. Kuchitira nkhanza munthu nzake kudzatha. Kudzakhala kukondwa pa tsikuli, kufuula kwa chimwemwe podzamvetsetsa komaliza; akubwera pafupi; ndikutha kuona angelo akiimba malipenga awo."

Mawu a lipenga akumveka mopfuula, kumwamba kukuwalirawalirabe, mpaka pamene sitingathe kuperira. Koma sitingasiye kuyang'ana pamenenso tizindikira; "Akundiona ine. Akundidziwa ine kuti ndine yani." Ndizazindikira ndi chimwemwe chachikuru "Uyu ndi Mulungu wanga akudzera ine, osatinso tsiku lina, koma panopa, lero."

Kodi mwakonzeka kudzamulandira mfumu mu ulemelero wake wonse? Ngati sichoncho, chonde, muitaneni Yesu panokha m'moyo mwanu tsopano lino. Monga kudza kwa Yesu kudzathetsa mavuto onse a padziko lapansi, kumulola iye kudza mumtima mwanu kudzakuthandizani kuthana nawo mavuto anu a tsiku ndi tsiku m'moyo uno. Uyu wamkulu wothetsa mavuto athu angakumasulen iku ku chitsutso ndi katundu wa tchimo ndi kukupatsani moyo wosatha.

Kubwera kwa Yesu m'moyo wa munthu kumasinthiratu kwakukuru ndi kwamuyaya, monga m'menenso kudza kwake kudzasinthire miyoyo yathu pa dziko lapansi. Inu mutha kumudalira Yesu. Adzakukonzetserani yekha pa zakubwera kwake ndi kukupatsani chitsimikizo chodabwitsa cha moyo wokondwa kwa muyaya.

KUMWAMBA NDIKO KWANU

Munthu wina dzina lake Marco Polo wa ku dziko la Venice anapita ulendo wa ku maiko a ku m'mawa. Iye pobwera kufika kwao anthu ankaganiza kuti wazungulira mutu - chifukwa amakamba za nkhani zodabwitsa.

Iye ankafotokoza kuti anaona m'mizinda ya siliva ndi golidi. Akuti anaonanso miyala ikuyaka moto; zobvala zoponyedwa pa malawi a moto koma osayaka; za njoka zikuluzikulu zotalika koposa 10 mamitala, zokhala ndi pakamwa poti zikhzoza kumeza munthu. Anakambanso za kuti anaona mtedza waukulu-ukulu okula ngati mutu wa munthu ndi nkhani zina zambiri. Anthu amangogwa nkuseka pomva nkhani ngati izi. Ndipo patapita zaka zambiri Marco Polo anadwala kwambiri munthu wina wotumikira Mulungu anabwera kudzamuona ndipo anamuua Marco kuti ayenera kulapa pa bodza lomwe wakhala akuwuza anthu asanatsikire kuli chete. Koma iye anayankha kuti "Zonse ndakhala ndikunena ndi zoona... Ndipo sindinanene ngakhale theka la zimene ndinaona."



Baibulo liri ndi zina zofanana ndi nkhani ngati imeneyi. Alembi a Baibulo poyang'ana kutsogolo m;masomphenya anafotokoza zochepa za zimene anaona. Iwo anaona zambiri m'Baibulo tipezamo zina za zinthu zina

1. KODI KUMWAMBA NDI MALODI ENIENI?

Yesu akukonza malo enieni a ife panopa kumwamba kwenikweni.

"Mtima wanu usavutike; mukhulupirira Mulungu, khulupirirani inenso (Yesu). Mnyumba ya atate wanga alimo malo okhalamo ambiri. Ngati sikudali kutero, ndikadakuuzani inu, pakuti NDIPITA KUKAKONZERA INU MALO. Ndipo ngati ndipita kukakonzera inu malo, NDIDZABWERANSO, ndipo ndidzalandira inu kwa Ine ndekha; kuti kumene kuli Ineko, mukakhale inunso." - Yohane 14:1-3.

Yesu akubweranso kachiwiri kudziko lino lapansi kudzatitengera kunyumba yokonzedweratu kumzinda woyerwa ndi waulemerero kumwamba, womwe sittingathe kuuganizira Yerusalemu watsopano. Titatha kukhala kumeneko zaka chikwi, Yesu akubweretsa mzindawo padziko lapansi pano. Ndiye pamene Yerusalemu watsopanoyu adzatsika, moto udzakhala utayeretsa dzikoli lonse. Dziko lathu lapansi lokonzedwanso mwatsopano lidzasandulika kwavo kwamuyaya kwa opulumutsidwawo. (Chibvumbulutso 20:7-15), izinso tizipeza zambiri mu phunziro la no. 25. Kodi Yohane, wolemba Chibvumbulutso, akuona zotsatiranso ziti?



"Ndipo ndinaona m'mwamba mwatsopano ndi dziko latsopano; pakuti m'mwamba moyamba ndi dziko loyamba zidachoka, ndipo kulibenso nyanja. Ndipo ndinaona mzinda woyerawo, Yerusalemu watsopano, ulikutsika kumwamba kwa Mulungu, wokonzeka ngati mkwatibwi wokometsedwera mwamuna wake. Ndipo ndinamva mau akuru ochokera ku mpando wachifumu

ndi kunena Taonani Chihema cha Mulungu Chiri mwa anthu; ndipo adzakhalitsa nao, ndi iwo adzakhala anthu ache ndi Mulungu yekha adzakhala nao, Mulungu wao." - Chibvumulutso 21:1-3.

Ndani adzalandire dziko lapansi losandulika?

"Odala ali akufatsa; chifukwa adzalandira dziko lapansi." - Mateyu 5:5 (Onaninso Chibvumbulutso 21:7).

Yesu akulonjeza adzabweranso dziko latsopano lokongola ngati Edeni wakaleyo, ndi anthu "Ofatsa adzalandira dziko lapansi".

2. KODI KUMWAMBA TIDZAKHALA NDI MATUPI ATHU OMWEWA?

Kodi pamene Yesu nauka m'manda naonekera kwa ophunzira ake, anati chiani za thupi lake?



"Onani manja ndi mapazi anga, ndine amene ndikuuzeni ndipo onani; mzimu sukhala ndi thupi ndi mafupa, monga mundionera Inemu." - Luka 24:39.

Yesu anali ndi thupi leni-leni ndipo anamuua Tomasi kuti amukhudze (Yohane 20:27) pa nthawi iyi nkuti Yesu nalowa m'nyumba yeni-yeni ndipo anayankhula ndi anthu eni-eni; nadya chakudya ndithu (Luka 24:43).

Kumwamba sikudzakhala mizimu koma anthu eni-eni amene amakondwera ndi moyo wauzimu koma matupi adzakhala ovala ulemerero.

"Pakuti ufulu wathu uli kumwamba, kuchokera komweko tilindira mpulumutsi, Ambuye Yesu Khristu; amene adzasanduliza thupi lathu lopepulidwa, lifanane nalo thupi lake la ulemerero, monga mwa machitidwe amene akhoza kudzigonjetsera nao zinthu zonse." - Afilipi 3:20, 21.

Inde matupi athu, monga thupi la Yesu poukitsidwa, lidzakhala leni-leni. Kodi nanga tidzawadziwa abale ndi abwenzi athu kumwamba? Inde.

"Pakuti tsopano tipenya m'kalirole, ngati chimbuuzi; koma pomwepo maso ndi maso tsopano kuzindikira mderamdera, koma pomwepo ndidzazindikiratu, monganso ndazindikirdwa." - 1 Akorinto 13:12.

Kumwamba tidzadziwadi zambiri tidzadziwa zakuya ndipo tidzayamika Mlengi. Ophunzira adalizindikira thupi laulemerero la Yesu (Luka 24:36-43). Mariya adadziwa Yesu pa tsiku louka kumanda chifukwa cha mau ake a Yesu (Yohane 20:14-16).

Ophunzira a Yesu pa njira ya ku Emau anamzindikira Yesu pamene lye anapempherera chakudya (Luka 24:13-35). Oomboledwa adzaonana maso ndi maso ndi anza! Kumwetulira kwa amuna anu, kaya akazi anu, amene namwalira mudzakuzindikira! Mudzawadziwa ana anu amene anamwalira kale pokumbukira zimene amachita ali ndi moyo pa dziko lapansi. Inde ngakhale abwenzi anu okondedwa mudzawadziwa! Inde kudzakhala chisangalalo chosatha!

3. KODI TIDZIDZACHITANJI KUMWAMBA?

Tidzakhala ndi zobetchera kumwamba? Kodi padzafunika kuganiza kumanga nyumba zathu zathu?

"Tamverani! Taonani, ndilenga kumwamba kwatsopano ndi dziko lapansi latsopano... ndidzasangalala mu Yerusalemu ndi anthu anga... adzamanga nyumba ndikukhalamo, adzabvala ndi kudya zipatso zake... anthu anga adzasangalala ndi ntchito ya manja ao." - Yesaya 65:17-22.

Yesu akutikonzera malo kumwamba aliyense payekha payekha - mu mzinda watsopano wa Yerusalemu (Yohane 14:1-3, Chibvumbulutso 21). Mavesi awa amatiuza kuti tidzamanga nyumba zokongola. Inde zoposa zimene timaziona lero ku mayadi.

Kodi mumakonda kuona mathithi a madzi kapena mumakonda nkhalango zokongola? Imvani izi:

"Yehova watonthoza mtima wa ziyoni, watonthoza mtima wa malo ake onse abwinja, ndipo wasandutsa chipululu chake ngati Edene..." - Yesaya 51:3.

Mulungu adzalitembenuza dziko kuti lioneke monga Edene wakaleyo. Sikudzakhalanso matope m'miseu yake, ngakhale nyansi zochokera m'mafakitole.

Udzakhala ngati m'banda kucha watsopano poona dziko latsopano-anthu a Mulungu adzakhalamo kwa tuyaya.

Kodi mumakonda zinthu zatsopano? Maphuziro? Kapena kuyambitsa zinthu zatsopano? Tamvani izi: "Maganizo mwa anthu oomboledwa mudzalowa mphamvu yoti adzamve zinthu za Umulungu... maganizo ndi malingaliro adzakula ... Tidzaphuzira maphunziro a nthano ya maomboledwe". - Great Controversy page 677, Ellen White.



4. KODI UCHIMO UDZAOPSEZANSO ANTHU OOMBOLEDWA?

"Ndipo simudzalowanso konse momwemo kanthu kali konse kosapatulidwa kapena iye wakuchita chonyansa ndi bodza; koma iwo okha olembedwa m'bukhu la moyo la mwana wa nkhosa." - Chibvumbulutso 21:27.

Mulungu ali wokonzeka kuthana ndi uchimo ndi zotsatira zake! Yesu akadzaoneka m'mitambo tidzamuona iye (1 Yohane 3:2). Tidzatsatira chiyero osati kukhunba kupha, bodza ndi chigololo.

"(Mulungu) ndipo adzawapukutira misozi yonse kuichotsa pamsao pao, ndipo sipadzakhalanso imfa: ndipo sipadzakhalanso maliro, kapena kulira, kapena chowawitsa, zoyambazo zapita." - Chibvumbulutso 21:4.

Ngakhale, mdani wathu wotsiriza, imfa idzakhonjetsedwa uko kumwamba anthu sadzafa (1 Akorinto 15:53) palibe ati adzakalambe!

Kumwamba sikudzakhalanso olumala zoyamba za m'dziko loipali zidzapita kwa tuyaya!

"Pamenepo maso a akhungu adzatsegulidwa ndi makutu a ogontha adzatsegulidwa. Pamenepo wopunduka adzatumpha ngati nswala, ndi lilime la wosalankhula lidzayimba pakuti chipululu madzi adzatuluka." - Yesaya 35:5, 6.

5. KODI CHOKONDWERETSA KOPOSA CHIDZAKHALA CHIANI KUMWAMBA?

Inde, kuonana ndi Mwini, Mbuye wa dziko lonse lapansi, chidzakhala chimwemwe choposa.

"Ndipo ndinamva mau akuru ochokera ku mpando wachifumu ndi kunena, Taonani, Chihema cha Mulungu chiri mwa anthu, ndipo adzakhalaitsa nao, ndipo adzakhala anthu ake, ndipo Mulungu yekha adzakhala nao, Mulungu wao." - Chibvumbulutso 21:3.



Mulungu wamphamvu akulonjeza kuti adzakhala nafe ndi adzakhala Mphunzitsi wathu. Taganizani zidzakhala zokoma motani! Ngati mwachitsanzo woyimba nyimbo afika pamaso mwini wopeka nyimbo!

"Ndipo kudzakhala kuti kuyambira pa mwezi wokhala kufikira pa unzake, ndipo kuyambira pa Sabata lina kufikira pa linzake, anthu onse adzafika kudzapembedza pamaso pa Ine, ati Yehova." - Yesaya 66:23.

Pakati penipeni pa mzinda woyeria pali mpando wachifumu wa Mulungu. Nkhope yozingidwa ndi utawaleza, anthu oomboledwa amasonkhana kupembedza Mulungu. Baibulo likuti.

"Ndipo oomboledwa a Yehova adzabwera nadzafika ku Ziyoni alikuimba; kukondwa kosatha kudzakhala pamitu yao, iwo adzakhala ndi kukondwa, ndipo chisoni ndi kuusa moyo kudzachoka." - Yesaya 35:10.

Nayu wina yemwe ukoma wake siutha. Iye ndiwokhulupirika ndiponso wopirira kosatha - lilemekezedwe dzina lake!

6. TIYENI TIKAPEZEKE KUMENEKO

Yesu akulakalaka kudzakomana ndi oomboledwa ake maso ndi maso. Nchifukwa chake analola kulipira dipo lalikuru pa mtanda. Inu mulandire nsembe iyi ndikubvomera kuti Yesu ndiye Mpulumutsi wanu, landirani chikhululukiro chochokera ku mtanda wa Yesu.

"Ndipo simudzalowa konse momwemo kanthu kali konse kosapatulidwa kapena iye wakuchita chonyasa ndi bodza; koma iwo okha olembedwa m'bukhu la moyo la Mwana wankhosa." - Chibvumbulutso 21:27.

Yesu amatiombola ku machimo osati mu machimo. Tiyenera ife kufika kwa lye kudzera m'mphamvu zake. Iye ndiye mau a pakamwa pathu mpakana akadza!



Ufumu wa Mulungu ukhoza kuyambira mu mtima mwanu. Yesu akatimasula ku uchimo, mu mtima mwathu mumakhala mtendere wa kumwamba. Kafukufuku wa posachedwa anaonetsa kuti anthu amene amakhala mu chiyemekezo cha Yehova amakhala moyo wokondwa kuposa anzao.

Palibe china chingakupangeni inu kukhala wokondwa kuposa kudalira mwa Mulungu. Tamvani zomwe Petro akunena za chikhulupiriro. Amene ngakhale simunamuona mumkonda, amene ngakhale simunampenya tsopano, pokhulupirira, ndi cha ulemerelo ndi kulandira chitsiriziro cha chikhulupiriro chanu, ndicho chipulumutso cha moyo wanu (1 Petro 1:8, 9).

Iyi ndiye mphotho yomwe Ambuye watikonzera kodi mukuona moyo waulere mwa Yesu! Mukumva kuitana kwake?

Ndipo Mzimu ndi mkwatiwbwi anena, Idzani. Ndipo wakumva anene Idzani. Ndipo wakumva ludzu adze, iye wakufuna, atenge madzi amoyo kwaulere (Chibvumbulutso 22:17).

Yesutu ali nanu tsopano, ndipo akulankhula ndi inu pamene mukuwerenga mau awa. Akukuitanani akuti, Idzani idzani, idzani! Inde akukulindirani! Ino ndiyo nthawi yabwino yomulandira!

Bwanji osamuza kuti mukulandira mphatso yomwe lye akupereka ndipo kuti mufuna kukakhala naye tuyaya? Muuzeni kuti mumukonda! Mthokozeni pa zimene wakuchitirani ndi zomwe wakukonzerani kuti akuchitireni! Kodi pali china chotchinga pakati pa inu ndi lye? Chichotseni! Lero pamene mukumva mau ake, dziperekeli kwa lye, weramitsani nkhopre yanu ndikupemphera kuti, Yesu Mbeye wanga ndibwera, ndikupatsani zonse. Ndikhale wanu nthawi zonse!

KODI KUBWERA KWA YESU KWAYANDIKIRA BWANJI?

Ambiri a ife takakamizika kufufuza za m'tsogolo. Tikufuna kudziwa zomwe ziri tsidya linalo, kutsogoloko. Koma chindunji chake cheni-cheni sichinapezekebe ayi. Tiri ndi nthawi yovuta ngakhale kudziwa kuti nyengo ya mawa ikhala yotani.

Koma alipo wina amene ulosi wake umachitikadi. Mwachindunji, Yesu Khristu, kupyolera m'Mawu ake, atha kutionetsera ife kutsogolo; ndi wotitsogolera wodalirika. Mu phunziro iri, tiona zomwe lye adanenapo za kubweranso kwake kwachiwiri. Ndiponsondani akadadziwa za kutsogolo kwadzikiko koposa lye amene analilenga dzikolo.

1. ZIZINDIKIRO ZA M'MASIKU ATHU ZOSONYEZA KUTI YESU ADZABWERANSO

Kodi Yesu atatha kuwatsimikizira ophunzira ake kuti adzabweranso kachiwiri ku dziko lapansi, (Mateyu 23:39), ophunzirawa adamufunsa kuti chiyani?

"Mutiuba ife zija zidzaoneka liti? Ndipo chizindikiro cha kufika kwanu n'chiyani, ndi cha matheude a nthawi ya pansi pano?" - Mateyu 24:3.

Yesu anawayankha momveka ndi mwachilimbikitso mu Mateyu mutu 24 ndi mutu 21 wa Luka. Iye akupereka yekha mwini "zizindikiro," kapena umboni umene ife tingadziwire kuti kudza kwake kwayandikira. Maulosi ena a m'Baibulo amathandizanso kukwanirtsia, ndi kutipatsa chinthonzi-thunzi cha m'mene tionere, maulosi amenewa akukwanirtsidwa tikuona ndi maso athu; kutitsogolera kuti kudza kwake kwa Yesu kwayandikira.



Tiyeni tione zikwangwani khumi za ulosi wa m'Baibulo zapanjira yathu yopita kumwamba, ndipo tifufuza ndi mafunso omwe munthu paulendo angadzifunse poona zikwangwani zapamsewuzo.

CHIKWANGWANI CHOYAMBA - ZOWAWA! CHISOKONEZO! MANTHA A AKURU!

Kuposera zaka 1900 zapitazo, Yesu anapereka za ulosi wa Khalidwe la moyo wakale ngati wotengedwa mu nkhanzi za madzulo:-

"Ndipo kudzakhala ZIZINDIKIRO pa duwa ndi mwezi ndi nyenyezi; ndi padzikola lapansi CHISAUKO CHA MTUNDU WA ANTHU, ALI NKUTHEDWA NZERU pa mkokomo wa nyanja ndi mafunde ache, ANTHU AKUKOMOKA NDI MANTHA, NDI KUYEMBEKEZERA ZINTHU ZIRI NKUDZA KU DZIKOLA LAPANSI; pakuti mphamvu za kumwamba zidzagwedezeza. NDIPPO PAMENEPO ADZAAONA MWANA WAMUNTHU ALINKUDZA mu mtambo ndi mphamvu ndi ulemelero waukuru. Koma moyamba kuchitika izi, weramukani, tukulani mitu yanu; chifukwa chiomboledwe chanu chayandikira." - Luka 21:25-28.



Palibe dongosolo linanso lomwe likanatha kulembbedwa la dziko lapansi la lero loposa loti. "Amuna adzakomoka ndi mantha, ndi kuyembekezera zinthu zirinkudza pa dziko lino." Zida zambiri zosonkhanitsidwa zitha kuononga dziko lapansi. Nanga kuli bwanji kuti

achifwamba atsogolere nkhondo yomenyera zida zamankhwala owopsa.

Yesu akutipatsa ife chiyambi cheni-cheni cha chiyembekezo mu nthawi ya matsoka ngati imeneyi. Nthawi yadziko imeneyi "ya chisauko ndi kuthedwa nzeru" zikungochitira umboni kuti kudzadi kwa Khristu "kwayandikira kwambiri." Anthu masiku ano akhudzidwa m'madandaulo, akukhumudwa. "Taonani m'mene dziko liliri tsopano! Koma ophunzira a ulosi wa mu Baibulo atha kufuula ndi mau a chiyembekezo, "Taonani iye amene akubwera kudziko lapansi."

CHIKWANGANI CHACHIWIRI - MATSOKA A M'DZIKO

Kodi zochitika zoononga zinthu m'dziko zikugwirizana bwanji ndi masiku otsiriza?

"Ndipo kudzakhala zivomezi zazikuru, ndi njala ndi miliri m'malo akuti akuti, ndipo kudzakhala zoopsy ndi zizindikiro zakumwamba... pakuona zinthu izi ziri kuchitika, zindikirani kuti ufumu wa Mulungu uli pafupi." - Luka 21:11, 31.

Tangoganizani za njala kwa kanthawi. Zithunzi-thunzi za ana omwe akufa ndi njala, mimba zawo zitalowa m'kat. Sizoziwitsa kuona kuti anthu a nzeru zopitira kumwezi akusowa nzeru zodyetsera anthu onse? Yesu anadziwa kuti njala idzapitilira ndi kuti anthu odzikonda okha adzapitilira kutero munthawi ya kumapeto kwa dziko.

Nanga bwanji za zibvomezi? Monga mwa kulemba kwa World Almanac" mu chaka cha 1999, akunena kuti nthawi ya zaka 100 ziri zone ya nyengo yakukhala akhristu, kwakhala kukuchitika zivomezi zikuru-zikuru: Mu zaka za zana chikwi ndi mphambu zisanu ndi zitatu (18th century), kunachitika zivomezi zisanu ndi chimodzi; muzaka zina za zana lotsatira apa (19th century) munachitika zivomerezi zisanu ndi ziwiri; ndipo m'zaka zina zana zotsatirazo (20th century), munachitika zivomezi zoposera zana limodzi. Choncho umboni wa izi ukunka nukula pamene tikufika m'masiku athu ano.



Chiwerengerochi chikukwaniritsa ulosi wa Yesu. Njala ndi zivomezi zazikulu zikufika pa chikati chawo cheni-cheni. "Ufumu wa Mulungu wayandikira." Kodi nanga m'badwo wathu uno udzabweretsa mazana ambiri a zivomezi zazikuru kapena kubwera kumene kwa Mfumu ya Mafumu?

CHIKWANGANI CHACHITATU - KUCHULUKA KWA CHUMA.

Kodi zitanthauzanji tikati chuma chidzakhala ndi anthu ochepta pamene ambiri adzakhala mu umphawi woopya.

"Mwadzikundikira chuma masiku otsiriza." - Yakobo 5:3.

Ngakhale dziko lonse lapansi liri pa vuto lachuma, olemera akunka nalemelerabe pamene osauka akunka nawonso nasaukirabe. Mipikisano ya mwayi ya ndalamala zambiri yomwe imachitika irinso zizindikiro zotionetsera ife kuti "kudza kwa Ambuye kwayandikira." (vesi 8).

CHIKWANGANI CHACHINAYI - KUSAKHUTITSIDWA PANTCHITO

Ndichifukwa chiyani kusakwanitsidwa ndi kuukira pa ntchito kwakula mofulumira kwambiri?



"Taonani; mphotho ya antchitowo anasenga m'minda yanu yozunguliridwa ndi inu powanyenga, ifuula, NDIPPO MAFUULO A OSENGAWO (ANTCHITO) adalowa m'makutu a Mbuye wa Makamu. Lezani mitima inunso, limbitsani mitima yanu, pakuti kudza kwake kwa Ambuye kuyandikira." - Yakobo 5:4, 8.

Atalosera za kudzikundikira chuma kwa mu nthawi yathu ino, Yakobo anaoneratu kusakhutira pa ntchito pakati pa olembewa chifukwa chosakhutitsidwa.

Chizindikiro chinanso choti "Yesu Ambuye ali pafupi kudza" ndicho kusagwirizana ndi kukokana-kokana pakati pa osauka ndi olemela.

CHIKWANGWANI CHA CHISANU - KUSWEKA KWA CHIKHALIDWE

Ndichifukwa chiyani chikhalidwe cha umunthu mudziko chikuoneka kuti chikuonongekerabe?

"Koma zindikirani ichi, kuti masiku otsiriza zidzafika nthawi zowawitsa. Pakuti anthu adzakhala odzikonda okha, okonda ndalamu, odzitamandira, odzikaza, amwano, osamvera akuwabala, osayamika, osayera mtima, opanda chikondi chachibadwidwe, osayanjanitsika, akudyerekeza, osakhoza kudziletsa, aukali, osakonda abwino, achiwembu, aliuma, olimbilira, otukumuka mtima, okonda zokondweretsa munthu osati okonda Mulungu; akukhala nawo maonekedwe a chipembedzo koma mphamvu yache adaikana... Koma anthu oipa ndi onyenga adzaipa chiipire, kusokeretsa ndi kusokeretsedwa." - 2 Timoteo 3:1-5, 13.



KWA MATSENZA

Kodi winanso angayembekeze dongosolo lina loposa apa? Lozetsani makina ojambula kulikonse padzikolo masiku ano ndipo mujambuleko zambiri. Mupezanzo zambiri zovuta kudzimvetsa zokhudza kuzunza ana. Mupezanzo zochita za ana zambiri zosathandizika, kupha ndi kuphana mwachisawawa ali ndi zaka zochepa. Zonsezi zikutipatsa chithunzi-thunzi choonetseratu poyera kuti kudza kwa Yesu kwayandikira.

CHIKWANGWANI CHACHISANU NDI CHIMODZI - KUFALIKIRA

Kodi ndi chifukwa chiyani kukhulupilira matsenga kwakula modabwitsa?

"Chifukwa akhristu onama adzakula, ndi aneneri onama nadzaonetsa zizindikiro zazikuru ndi zozizwa koteru kuti akanyenge, ngati nkotheka osankhidwa omwe." - Mateyu 24:24.

Ndime izi zikulosera kuti munthawi yakumapeto kudzaonekera zozizwa ndi zizindikiro zambiri zoonetsera ngati zochokera kumphamvu yodabwitsayo. Mfiti ndi anyanga adzaonekera paliponse, kugulitsa zithumwa zaho, kulumikizana polankhula ndi mizimu. Zizindikiro zofanana ngati zoona ndi zozwizwa zidzauka. Zonsezi zikuchitikira umboni monga Khristu analosera, kuti, tikukhala mu nthawi ya "kudza kwa mwana wa munthu." (vesi 27).

CHIKWANGWANI CHA CHISANU NDI CHIWIRI - KUDZIDZIMUTSIKA KWA DZIKO

Kodi zikutanthauzanji tikati kudzidzimutsika kwa kudziko - kutsitsimuka kwa Africa, kwa maiko a kum'mawa, pakati kum'mawa kwa Ulaya ndi maiko a kutali uko kum'mawa?

"AGALAMUKE AMITUNDU;... Longani zenga, pakuti dzinthu dzacha... Pakuti zoipa zao nzazikuru. Aunyinji, aunyinji m'chigwa chotsiriza mlandu! Pakuti layandikira TSIKU LA YEHOVA M'chigwa chotsiriza mlandu." - Yoweri 3:12-13.

Lero ku Asiya ndi ku Afrika, kum'mawa kwa Ulaya ndi komwe kale kumatchedwa Soviet Union, komanso maiko a pakati ku m'mawa, tonse tikuchitira umboni izi za kudzidzimutsika kwa maiko aliwonse paokha-paokha zonse monga mwa ndondomeko ya momwe mbiri yakale ikunenera, "pakuti tsiku la Ambuye layandikira."

CHIKWANGANI CHA CHISANU NDI CHITATU - ZILINGANIZO ZA MTENDERE NDI KUKONZEKERA NKHONDO

Tikukhala ife m'dziko la chilendo. Aliyense akuvomereza kuti payenera pabwere mtendere. Timanena za mtendere; koma ziwawa zilipo zambiri ndipo zinayamba kale-kale. Aneneri monga Mika ndi Yoweri analosera kuti munthawi yomwe maiko adzakambirana za mtendere (Mika 4:31), kusakhulupilirana kwa maiko kudzabuka koma kudzanso nkhondo pakati pa maiko oyandikana (Yoweri 3:9-13).



Kalelo Baibulo limaonetsera momwe dziko latsopanoli lomwe tikukhalali lidzakhalira lofuna mtendere - komanso lankhondo, ndikuonetsa kuti mtendere sudzatheka mpaka pamene Yesu adzabwere.

CHIKWANGANI CHA CHISANU NDI CHINAYI - KUCHULUKA KWA NZERU

Ndichifukwa chiyani, patatha zaka zambiri mumbiri ya dziko lapansi, kuti mtenga-tenga ndi mtokoma kwapangitsa ngati maiko ali pafupi-pafupi?

"MPAKA NTHAWI YA CHIMALIZIRO; ambiri adzathamanga chauko ndi chauko, ndi chidziwitso chidzachuluka." - Daniel 12:4.

Apa Daniel akusonyezera kuti nzeru za ulosi wake zidzachuluka "mu" kapena "mpaka nthawi ya kumapeto." Koma ulosiwu ukulozeranso chindunji cha nthawi yathu ino ya makina a kompyuta. Nzeru za mtundu wina uli wonse zapita pa tsogolo mwa kuthwanima kwa mphezi m'zaka zochepa zokha zapitazo. Kwakhala kusintha kwakukuru mzaka makumi asanu okha zomwe zapitazo, poyelekeza ndi kusintha komwe kwachitika mu zaka zikwi zikwi zapitazo.

"AMBIRI ADZAPITA UKU NDI UKO, kuonjezera nzeru." Chisanafike chaka cha 1850, anthu ankayenda pa ngamira, ndi a bulu ndi nyama zina zomwe anali nazo pa nthawi yawo kuyambira pachiyambi. Koma lero, maulendo akuyendedwa pa ndege zikulu-zikulu mu mlenga-lenga.

Kuchuluka kwa maulendo ndi kusefukira kwa kufufuza mwaukatswiri kutipatsa umboni wokwanirtsa kuti tiri kukhala mu "nthawi ya kumapeto."

CHIKWANGANI CHA CHIKHUMI - UTHENGA WABWINO KUDZIKO LONSE LAPANSI



Yesu analosera kuti atangotsala pang'ono kuti akubweranso, uthenga wabwino udzalalikidwa ku dziko lonse lapansi.

"Ndipo uthenga uwu wabwino waufumu, udzalalikidwa pa dziko lonse la pansi, ukhale umboni kwa anthu amitundu yonse ndipo pomwepo chidzafika chimaliziro." - Mateyu 24:14.

Kwa zaka zambiri, pafupi-fupi theka la dziko lapansi linatsekeredwa mu mdima, kutari ndi uthenga wabwino. Koma ndithu mwadzidzidzi

mukanthawi kochepa, kum'mawa kwa Ulaya kunacha kumasulidwa kwa nsinga za komyunisiti. Khoma la Berlin linanka ligwa ndi ufumu wake unayamba kugawanika mwadzidzidzi pafupi-fupi theka ladziko lapansi linatambasuka m'manja kulandira uthenga wabwino.

Uthenga wabwinowu ukupitadi "kudziko lonse lapansi" kuposa momwe sunachitikirenso. Kupyolera pa Kanema, uthenga ukufalitsidwa pafupi-fupi dziko liri lonse. Tikukhala m'masiku awodi omwe Yesu ananena m'mene anati: "Uthenga uwu wabwino udzalalikidwa ku dziko lonse lapansi" ndipo "pamenepo chimaliziro chidzafika."

2. KODI PAYANDIKIRA BWANJI PAKUDZA PACHE PA YESU

Atatha kulongosola zochitika zomwe zidzaonetsera kudzanso kwake, Yesu anamaliza ndi mau otí:

"Indetu ndinena kwa inu, m'badwo uwu sudzatha kuchoka, kufikira zinthu zonsezi zidzachitidwa." - Mateyu 24:34.

Kumalizaku nkodziwikiratu - m'badwo womwe ukunenedwa ndi zizindikirozi za ulosi udzaona Yesu akubweranso kachiwiri ku dziko lapansi. Sipadzakhalitsa, ndipo adzachotsa tchimo lonse, ndi kuzunzika konse, ndikukhazikitsa ufumu wake wamuyaya. Yesu akuchenjeza, "palibe aliyense yemwe adziwa... tsikulo kapena nthawi yake - (vesi 36). Ndipo Yesu akupitiliza kunena kuti:

"Chifukwa chake khalani inunso okonzekeratu; chifukwa mu nthawi imene simuganizira, Mwana wamunthu adzadza." - Mateyu 24:44.

3. YESU, CHIYEMBEKEZO CHOKHALA CHA DZIKO LAPANSI

Yesu ndiye chiyembekezo chomaliza chopambana ku dziko lathuli lapansi, chifukwa ndi lye yekha yemwe angaononge tchimo lomwe lasautsa dziko lapansi. Yesu anafa pa Karavali kuti kukakhale kotheka kugonjetsa choipa ndi kumasula onse amene avomera chipulumutso chomwe lye wachipereka.

"Iye wochita tchimo ali wochokera mwa m'dierekezi, chifukwa m'dierekezi anachimwa kuyambira pachiyambi. Kukachita ichi Mwana wa Mulungu adaonekera, ndiko kuti akaononge ntchito za m'dierekezi." - 1 Yohane 3:8.



Mpulumutsi wathu anakonza njira kuti dziko likamasukire podzipereka thupi lake lomwe ndi mwazi wake nsembe, Ndipo Yesu yemweyo, yemwe tsiku lina adzachiritsa dziko lonse ku tchimo ndi zotsatira zake, akuperekanso mwayi wochiritsa miyoyo yathu ya tchimolo.

Simuyenera inu kudikira kuti abwerenso kachiwiri kuti moyeretsedwe ku tchimo, kapena kuti musiye makhalidwe achionongeko ayi. Yesu ali wolola kukupatsani mtendere wake pompano.

Msungwana wina wake, ankachita nawo msonkhano wauzimu. Anakhudzidwa ndi uthenga womwe umalalikidwawo. Pamene anamva nthano ya kubweranso kwachiwiri kwa Mpulumutsi ikuvumbulutsidwa, anaona kuti zizindikiro zonse zikugwirizana.

Anaona kuti zikupanga zinthu kukhala zomveka bwino. Kenaka adapeza kuti iye ankafuna-funa chikondi, kukondwa ndi mtendere ku malo



olakwika. Yesu ndi wolola kutipatsa mtendere pompano.

Tsiku linzakelo pamene wolalikirayo ndi gulu lake adamuyendera, adawauza bwino lomwe za moyo wake wosautsa umene adakhala nawo. Anawauza kuti adali chidakwa, ndipo ankachita zachiwere-were kuti apeze zosowa zake. Atatha kulongosola mavuto ake adayamba kukhetsa misozi, nanena, 'usiku uja mumalalika za m'mene ine ndiriri ndithu."

Koma mawu omwe adamukhudza iye adali mawu a Mulungu, ndipo amamuyankhula mofatsa. Ndipo iye adafika pogoniza zosiya zonse namuitana Khristu kulowa mumtima mwake monga Ambuye ndi Mpulumutsi wake, nagwiritsitsa ku chiyembekezo cha kubweranso kwachiwiri kwa Yesu Khristuyo.

Mu masabata otsatira apo, iye adayamba kuona kuti mantha ndi kusowa chitetezo kwake kwakukulu komwe amakubisalira mukuledzera, kunamasulidwa pamene nthawi yambiri tsopano ankalumikizana ndi Yesu. Yesuyo adayamba kumumasula iye kuzonse zomwe zimasautsa moyo wake.

Adachita iye zambiri zomwe sanathe kuti angazinyadire koma chifundo ndi chisomo komanso chikhulupiliro cha Khrisu chinaonetsera mphamu zazikuru koposera manyazi ake. Omwe adaona mbava ya pamtanda zinali ndi tanthauzo lalikuru kwa iye. Mu nthawi yake yazowawa yakumapeto, adatembenukira kwa wolangidwa wosalakwayo yemwe anali pambali pake napempha, "Yesu, mundikumbukire ine pamene mudzadza mu ufumu wanu" (Luka 23:42). Yesu anamuyankha pomwepo namulonjeza iye malo kukhala naye ku Paradizo (Vesi 43).

Yesu yemweyo anakhululukira mwa chisomo kwa mbava ija yomwe inafa, akuperekanso tsopano kwa inu chipulumutso, kukhulukira konse, ndi mtendere mumtima. Dzipezereni inu nokha lero zinthu zimenezi.

Inunso mungathe kupemphera ngati mbava yophedwa pamtanda ija kuti: "Yesu, mundikumbukire ine pamene mudzadza mu ufumu wanu." Ndipo Yesu adzayankha, "Ndidzabweranso, ndipo udzakhala ndi Ine ku Paradizo."

MPHAMVU YODABWITSA M'MOYO WANGA

Muchaka cha 1929, munthu wina wotchedwa Frank Morris adakwera nawo Sitima yapanyanja yopita ku Switzerland. Ulendo umenewu ankaudikilira kwa nthawi yaitali. Koma unali ulendo wosautsa. Yemwe anali womutumikira mu sitimayo ankamutsekera iye mukachipinda usiku uli wonse. Atatha kudya chakudya cham'mawa mofulumira, Frank ankatha kuchita masewera olimbitsa thupi pang'ono, koma samamva kumasuka kuti adzichitidwa monga ngati chiweto kuti adzitsogoleredwa kuzungulira sitimayo. Kenaka womuyang'anirayo anamukhazika iye pa mpando wa mu sitimayo. Nthawi zonse pamene adakumana ndi wokwera sitima wina yemwe anali ngati bwenzi namuitanira kukayenda woyang'anirayu adamukaniza nanena kuti iye waikidwa kumuyang'anira iye mosamalitsa.



Frank anali wamkulu, wachidwi ndi zofuna ngati munthu wamkulu. Komanso anali wosaona, ndipo womutumikirayu adaona kuti Frank sangadzitumikire yekha. Frank anali ngati katundu wopangidwa ndi kutumizidwa mopanda iye kunenapo kanthu.

Koma atafika ku Switzerland, moyo wa Frank udasintha modabwitsa. Ali komweko adaphunzira kuti panali galu ophunzitsidwa bwino kutsogolera anthu akhungu. Pomubweretsa m'busa wina wa ziweto wa ku German wotchedwa Buddy ku America kunapangitsa Frank kuyambitsa bungwe lalikulu pa dziko lonse lapansi loona za maso.

Ndi Buddy, pambali pake, Frank anatha kupita pali ponse, nthawi iri yonse ndi ali yense. Ndipo anali womasuka tsopano. Nthawi ina, ali pachionetsero kwa atolankhani pa msewu wina wodutsa magalimoto ndi zokwera zambiri mu mzinda wa New York , Buddy adamutsogolera mbuye wake mwa luso kuchoka mu msewu wina kupita msewu winanso, pamene magalimoto ambiri akudutsanso mwaliwiro. Chifukwa chomudalira ndi kumukhulupirira Buddy kwambiri, Frank adadutsa misewu mosavuta. Atolankhani adavutika kudutsa mpaka wina wa iwo adapeza galimoto ndikukwera kuti apite mbali ina.

Mu ndime zotsatirazi, tiphunzira za Mzimu woyer, wotsogolera amene amafuna ife kuti tiike miyoyo yathu m'manja mwake. Tonsefe ndife wolumala mwa umunthu, khungu tiri nalo ku zinthu zomwe ziri zofunika. Ndipo nthawi ya moyo wathu iri yofulumira kwambiri moti tinangopezeka kuti tikungotsatira zinthu zina, m'malo mopita chitsogolo. Ndipobe, tiri okaikira kuti tikhulupilire miyoyo yathu kwa wina wake kuti atitsogolere. Koma chofufuzidwa chopezeka chenicheni chikutidikirira ife ndi ichi: tidzapeza ufulu weni-weni ndi mphamvu pozamitsa chidaliro chathu pa Mzimu woyer, kuti atitsogolere ife moyo wathu wonse.

1. WOIMIRA KHRISTU M'DZIKO LAPANSI

Pamene Yesu anali pafupi kukwera kunka kumwamba, anawalonjeza ophunzira ake mphatso yaulere:

"Koma ndinena Ine choonnadi ndi inu, kuyenera kwa inu kuti ndichoke Ine; pakuti ngati sindichoka, NKHOSWEYO sadzadza kwa inu; koma ngati ndipita ndidzamtuma lye kwa inu... Koma atadza lyeyo, MZIMU WA CHOONADI, adzatsogolera inu m'choonadi chonse... IYEYO ADZALEMEKEZA INE; chifukwa adzatenga za mwa Ine nadzalalikira kwa inu." - Yohane 16:7, 13, 14.

Mu chikonzetsero choyeracho, Yesu anayenera kubwerera kumwamba ngati wotiimilira kwa Mulungu, naonekera m'malo mwa ife pamaso pa mpando wake wa Mulungu" (Ahebri 9:24). Pamene Ambuye wathu wopachikidwayo akutiimilira



kumwamba, tirinso ndi NKHOSWE ndi WOTITSOGOLERA, ndiye Mzimu woyerera, pansi pompano. Iye ndiye woimilira Yesu Christu.

Ali padziko lapansi pano, Yesu adatumikira mbali zonse za thupi la munthu, ngakhale sanathe kupeze ka pali ponse. Koma mzimu woyerera alibe malire; atha kutumikira ngati nkhoswe ndi mtsogoleri kwa anthu osawerengeka ku malo ambiri nthawi imodzi. Christu amathetsa zosowa zathu kupyolera mwa mzimu woyerera.

2. KODI MZIMU WOYERA NDI NDANI?

Ambiri aife tingathe kulumikizana ndi Mulungu Atate ngati titathanso kuganizira, chisamaliro chomwe lye amatipatsa chomwe sichinaonekenso ndi kale lonse, lye ngati kholo lathu. Ndipo titha kuona Yesu Mwana Wake, chifukwa anakhalanso lye monga munthu ngati ife mudzikolo lomwe lino. Koma Mzimu woyerera, ndikovuta kuika pa chithunzi-thunzi chake ndi kuyerekeza kwake. Tiribe chamunthu chomwe tingayerekezere ndi mzimu woyerera, komabe Bukhu lopatulika limatipatsa ife dongosolo leni-leni la Mzimu woyerera.

KHALIDWE: Yesu anayerekeza Mzimu woyerera monga munthu m'modzi wa atatuwo mu uMulungu, wokhala nawo pamodzi ndi Mulungu Atate ndi Mulungu Mwana.

"Chifukwa chake mukani, phunzitsani anthu a mitundu yonse, ndikuwabatiza iwo m'dzina la ATATE, ndi la MWANA, ndi la MZIMU WOYERA." - Mateyu 28:19.

Mzimu uli ndi khalidwe lake-lake: maganizo (Aroma 8:27); nzeru (1 Akorinto 2:10); chikondi cha kwa ife (Aroma 15:30); kutha kutiphunzitsa (Nehemiya 9:20); kumva chisoni pamene tichimwa (Aefeso 4:30); ndi mphamvu yakutsogolera.

KUKHALA NAWO PA CHILENGEDWE: Mzimu woyerera anali nawo pachilengedwe cha dziko lapansi pamodzi ndi Atate ndi Mwana.

"PACHIYAMBI Mulungu adalenga kumwamba ndi dziko lapansi... ndipo MZIMU WA MULUNGU unalinkufungatira pamwamba pa madzi." - Genesis 1:1, 2.

3. NTCHITO ZA MZIMU WOYERA



(1) Kusintha mtima wa munthu. Pamene adakumana ndi Nikodimo, Yesu adatsimikizira mbali yomwe Mzimu woyerera amachita pakusintha mtima wa munthu.

"Yesu anayankha nati, 'indetu, indetu ndinena ndi iwe, ngati munthu sabadwa mwa madzi ndi mzimu, sakhoza kuona ufumu wa Mulungu.'" - Yohane 3:5.

Kubadwa "mwa Mzimu" zitanthauza kuti Mzimuyo amatiyambitsa moyo watsopano. Sikungosintha makhalidwe athu kokha ayi, koma kusinthika kwa m'kati ndi kunja komwe, kukwaniritsa malonjezo oti:

"Ndidzakupatsani inu mtima watsopano (Ezekiel 36:26).

(2) Kutidziwitsa ife zoipa zomwe tachita ndikutipatsa chikhumbo-khumbo cha chiyero.

"Ndipo atadza lyeyo (Mzimu Woyerera) ADZATSUTSA DZIKO LAPANSI za machimo, ndi za chilungamo, ndi za chiweruzo." - Yohane 16:8.

Mukamva za nthano za wina yemwe adasinthika modabwitsa kuchoka ku moyo watchimo kupita kwa Mulungu nakhala m'banja wokhulupirika ndi kholo losamala, kumbukirani kuti khwerero liri lonse adatenga, lidadza ndi kudandaulira kwa Mzimu woyeria.

(3) Kutitsogolera ife m'moyo wathu wachikhristu. Yesu analankhula nafe mwachindunji kupyolera m'mawu aang'ono "akachete-chete" a Mzimu.

"Ndipo makutu ako adzamva mawu kumbuyo kwa iwe akuti, 'njira ndi iyi, yendani inu m'menemo.'
Potembenukira inu ku lamanja, ndipo potembenukira ku la manzere." - Yesaya 30:21.

Kupyolera pa Kanema, zinthu zambiri zakutali ku dziko lonse lapansi taziona pafupi ndi maso athu. Mzimu woyeria amakhala ngati uthenga wa pakanema wa Mulungu, kumubweretsa Yesu pafupi kuchokera kumwamba kudza kudzikola lapansi, ndikumupanga lye wopezekeratu panthawi iri yonse imene timufunitsitsa (Yohane 14:15-20).

(4) Kutsogolera moyo wa mapemphero.

"Ndipo momwemo MZIMU ATHANDIZA KUFOOKA KWATHU pakuti chimene tizipempha monga chiyero; sitidziwa; koma Mzimu mwini atipempherera ndi zobuula zosatheka kuneneka... monga chifundo cha Mulungu." - Aroma 8:26, 27.

Pamene tivutika kupeza mawu, Mzimu amapemphera m'malo mwathu. Pamene takhumudwitsidwa, tingathe kulilira kwa Mulungu kokha, ndipo Mzimu amakulitsa chikhulupiliro cha kulira kwathu kuchoka mukuchepa kwake kufikira ku pemphero lamphamu lofikiratu pa mpando wake wachifumu wa Mulungu kumene Yesu ali kutumukira.

(5) Kukuza makhalidwe ndi maonekedwe a Chikhristu. Mzimu amapangitsa anthu opanda chipembedzo kukhala obala zipatso zauzimu.

"KOMA CHIPATSO CHA MZIMU ndicho chikondi, chimwemwe, mtendere, kuleza mtima, chifundo, kukoma mtima, chikhulupiliro, chifatso, chiletso, pokana zonzezi palibe lamulo." - Agalatiya 5:22, 23.

Kukhala ndi mphatso za Mzimu zimaonetsera kuti ife tiri m'nthawi yolumikizidwa ku mpesa weni-weni, Yesu (Yohane 15:5). Yesu atha kukhala moyo wake wonse mwa ife kupyolera mwa Mzimu woyeria ndi mphamu zake.

(6) Kutikonzetsera ife kukhala mboni. Yesu akulonjeza:

"KOMATU MUDZALANDIRA MPHAMVU, Mzimu woyeria atadza pa inu, ndipo mudzakhala MBONI... kufikira malekezero ache a dziko." - Machitidwe 1:8.

Onse omwe ali olola, angathe kukhala mboni motsogozedwa ndi Mzimu. Sitingathe ife kukhala ndi mayankho, koma Mzimu adzatipatsa mayankho ndi nthano zomwe zidzatha kusintha mitima ndi maganizo a anthu. Atumwi anali ndi vuto kuti amvane pa tsiku la Pentekosite, koma Mzimu woyeria atabwera, adanena ndi mphamu, za Yesu Khristu mpaka "adalitembenuza dziko chadololido. (Machitidwe 17:6).

4. MPHATSO ZA MZIMU WOYERA

Mawu a Mulungu akulekanitsa momveka bwino pakati pa Mphatso ya Mulungu ya Mzimu woyeria kwa aliyense kuti akhale MIKRISTU wopambana m'moyo; ndi mphatso zosiyana-siyana zomwe Mzimu anapereka kwa wokhulupilira kuti atumikire mwapadera mwa njira zosianasiyana.



"Chifukwa chake ananena, m'mene anakwera (Khristu) kumwamba, anamanga ndende undende, namuika za ufulu kwa anthu.... Ndipo lye anapatsa ena akhale ATUMWI, ndi ena ANENERI, ndi ena ALALIKI, ndi ena ABUSA, ndi ena APHUNZITSI, kuti akonzere oyera mtima ku ntchito ya utumiki kumangilira thupi la Khristu." - Aefeso 4:8, 11-12.



Mkhristu m'modzi salandira mphatso zonzezi ayi. Ena atha kulandira zingapo kuposera anzawo. Mzimu Woyer "amaperekwa kwa iwo molingana ndi m'mene lye Mzimuyo akuonera" (1 Akorinto 12:11). Mzimu woyer amamuzamitsa wokhulupilira aliyense mu ntchito yake malinga ndi chikonzetsero cha Mulungu. Mulungu amadziwa nthawi ndi malo kumene kufunikira mphatso iri yonse kuti zikalitse anthu ake ndi Mpingo wake.

Mum'ndandanda wina wa mphatso za mzimu woyer ukupezeka pa 1 Akorinto 12:8-10 ndipo zina za izo ndizo nzeru , chidziwitso, chikhulupiliro machiritso, ulosi, kulankhula malilime osiyana-siyana (manenedwe, zilankhulo), ndi kutanthauzira kwa malirimewa (vesi 8-10).

Paulo akutiumiriza ife kuti "tikhumbe modziperekwa ndi mofunitsitsa mphatso zimenezi," ndipo akunenanso kuti, "ndipo tsopano ndidzakuonetserani inu njira yopambana zonse" (1 Akorinto 12:31).

Mutu wonena za chikondi (1 Akorinto 13) umene ukubwera patsogolo pa vesili umatsimikizira kuti, "njira yopambana zonse," ndiyo njira ya chikondi. Ndipo chikondi ndi mphatso ya Mzimu (Agalatiya 5:22).

Ife tiyenera kukhudzidwa ndi kufuna-funa mphatso za Mzimu ndi kulola Mzimuyo kutigawira ife mphatsozo monga momwe "lye afunira" (1 Akorinto 12:11).

5. KUKWANIRA KWA MZIMU PA PENTEKOSITE



Pa tsiku la Pentekosite, Mzimu woyer adatsanulidwa mopanda malire, kukwaniritsa lonjezo la Yesu:

"Komatu mudzalandira mphamvu, Mzimu woyer atadza pa inu; ndipo mudzakhala mboni zanga... kufikira malekezero ake adziko." - Machitidwe 1:8.

Pa Pentekosite, Mzimu anapangitsa atumwi kufalitsa uthenga momveka bwino mu ziyankhulo za mtundu wina uli wonse wa anthu "a dziko liri lonse la pansi pa thambo" (Machitidwe 2:3-6).

Ophunzira a Bukhu lopatulikali ambiri amayerekeza kudza kwa Mzimu woyer kumeneku ndi mvula yoyambilira ya nyundo ndi mvula yotsiliza ya masika ya ku Palestina (Yoweli 2:23).

Mzimu yemwe adabwera pa Pentekosite anali ngati "Mvula yoyambilira" ya nyundo yomwe imameretsa mbeu naiperekwa chakudya chofunikira ku mpingo wa Khristu mu Chiyambi chake.

6. MVULA YOTSIRIZA YAMASIIKA YA MZIMU WOYERA

Ulosi wa m'Bukhu lopatulika umatiuza za tsiku likubwera pamene Mzimu wa Mulungu udzatsanulidwa ku mpingo wake ngati mvula, kuwapatsa anthuwo mphamvu, kuti akachitire umboni (Yoweli 2:23).

Zaka zambiri zadutsa ndithu pamene nthano ya chipulumutso yafalitsidwa ku mbali yaikulu ya dziko lapansi. Ndi nthawi ino tsopano kuti "mvula ya Masika" ichetse mbewu, kuzikhwimitsa, kuti zikathe kukololedwa.

Pamene mbiri ya dziko lapansi ikufika pachimake peni-peni, Yesu asanabwere, Mulungu adzakonzetsera wokhulupilira aliyense, kupyolera mu mphanvu yaikulu ya Mzimu woyer, kuti akalowe kumwamba. Kodi inu mutha kuona mphamvuyi ya "mvula yoyamba" yokonzetsera mpingo ku "mvula yamasika" ya Mzimu woyer? Kodi mukukhala inu m'moyo wodzadzidwa ndi Mzimu? Pamene mulimbikitsidwa inu ndi Mzimu, mungalole kodi Mulungu kukugwiritsani ntchito yofalitsa za chikondi chake choposa ndi kudza kwake kwa posachedwa?

7. ZOYENEREZA MUNTHU KULANDIRA MZIMU WOYERA

Pa Pentekosite, Mzimu woyer anakhudza iwo amene anamva Mawu a Mulungu, nadzifunsa molira kuti, "kodi abale, tidzachita chiyani?" (Machitidwe 2:37).

"Koma Petro anati kwa iwo, 'LAPANI, BATIZIDWANI yense wa inu m'dzina la Yesu Khristu kuloza ku chikhululukiro cha machimo anu, ndipo MUDZALANDIRA MPHATSO YA MZIMU WOYERA.'" - Machitidwe 2:38.

Kulapa - kuchoka ku njira za uchimo ndi kubwelera kwa Khristu, ndyo njira imodzi yoyenera kulandira mphatso za Mzimu woyer. Kuti Mzimu atsanuliridwe pa ife, tiyenera kuyamba talapa ndi kuipereka miyoyo yathu kwa khristu. Yesu anatsimikiziraponso pa za kufunitsitsa kum'tsatira lye ndi kumumvera lye ngati njira ina yotiyenereza ife kulandira mphatso za Mzimu woyer (Yohane 14:15-17).



8. MOYO WODZADZIDWA NDI MZIMU

Yesu asanachoke pa dziko lapansi, anawalangiza ophunzira ndi omutsatira ake motere:

"Musachoke mu Yerusalem, komatu mulindire lonjezano la Atate, limene anati, munalimva kwa Ine... pakuti Yohane anabatizadi ndi madzi; koma inu mudzabatizidwa ndi Mzimu woyer, asanapite masiku ambiri." - Machitidwe 1:4, 5.

Posanthula-santhula m'Bukhu lopatulika tisonyezedwa kuti Mkhristu ayenera "kudzadzidwa ndi Mzimu woyer" (Machitidwe 2:4; 4:8; 4:31; 6:3; 6:5; 7:55; 9:17; 13:9; 13:52; 19:6). Mzimu woyer umapangitsa moyo wamunthu kukhala wokwaniritsa ndi wabwino chifukwa moyo wodzadzidwa ndi Mzimu umafikiritsa mbendera zonse zomwe Khristu ali nazo pa ife.

Pamene tikulongsola za moyo wodzadzidwa ndi Mzimu wa chikhristu, Paulo akupereka pemphero iri loti likanenedwe ndi wokhulupilira aliyense:

"Kuti monga mwa chuma cha ulemelero wake akulimbikitseni inu ndi mphamvu mwa Mzimu wake, m'kati mwanu, kuti Khristu akhale chikhaliire mwa chikhulupiliro m'mitima yanu,... Ndipo kwa iye amene angathe kuchita koposa -posatu zonse zimene tizipempha, kapena tiziganiza, monga mwa mphamvu ya kuchita mwa ife." - Aefeso 3:16, 17, 20.

Monga Frank Morris ndi galu wake wokhulupirika pomutsogolera, Buddy, ifenso motsogozedwa ndi Mzimu woyer m'kati mwathu, titha kuchita zinthu zambiri zosawerengeka zomwe sitinachitepo ndi kale

lomwe. Ndi zikhumbo zatsopano ndi mphamvu zatsopano, ife titha kupita chitsogolo molimba mitima m'malo mongoyesa kuti tithane ndi zovuta za m'moyo.



Machita-chita odzadzidwa ndi Mzimu amapangidwanso mwatsopano tsiku ndi tsiku kupyolera mupemphero ndi kuphunzira mawu a m'Bukhu lopatulika. Pemphero limatiika ife pafupi zedi ndi Khristu pamene kuphunzira mawu a m'Bukhu lopatulika kumatipanga ife kuyang'ana kwambiri kwa lye munjira zathu zonse. Izi zimaphwanya malinga onse otitchingira ife ndi Yesu Khristu kuti asatitsanulire mphatso zathu zaulele za Mzimu. Umu ndimo m'mene tikhalira, ndikuchotsa makhalidwe akale oipa ndikuikamo maonekedwe aukhondo a khalidwe lathu.

Aroma 8 amatilongoslera ife bwino maonekedwe a moyo wodzadzidwa ndi Mzimu. Pezani nthawi yanu muwerenge pamene mungathe, ndipo muwerenge kuti ndi nthawi zingati zomwe Paulo akulozera ku "Mzimu" monga mphamvu yokhayo ya moyo wachikhristu.

Kodi inu mwafufuza zozizwa zopezeka mu moyo wodzadzidwa ndi Mzimu? Ndinu wofunitsitsa kuti Mzimuyu akhale m'moyo mwanu? Kodi mwayamba kale kuona mphamvu yake yopatsa moyo? Tsegulani mitima yanu kumphamvu yaikuru iyi yomwe iri m'dziko lonse.

MPULUMUTSI WOPEZEKERATU NTHAWI IRI YONSE



Pamene kam'nyamata kena kake ka mdziko la Scotland kochedwa Petro kanasowa usiku wina wamdimma waukuru ku chire lina lake kumeneko lochedwa Wasteland, Mulungu anamuitana dzina lake; "Petro". Pamene mau akumwambawa adaitananso Petro anaima mukanjira kena kake, nayang'ana pansi, napeza kuti anatsala pang'ono kuti agwere mu ngalande yaikuru yomwe inakumbidwa ndi oswa miyala.

Kodi sizikadakhala zabwino kwambiri kuti aliyense wa ife amve kuitana kwa Mulungupa dzina lake? Sizikanakhala zabwino kuti Mulungu akhale bwenzi lathu lapafupi - ife titangoti tikhale pansi naye pamodzi ndi kucheza naye nthawi yaitali pa za mavuto ndi maloto athu?

1. MWAYI WOPANDA MALIRE WOLUMIKIZANA NDI YESU

Kaya mufuna kuti mukhulupirira, kaya ayi, koma dziwani kuti titha kudza chifupi ndi Yesu panopa koposa mmene zinaliri nthawi yomwe lye anali m'dziko lapansi nafe, wooneka mwa umunthu. Kukhala ndi Yesu mwa thupi mdera lathu, ndi chinthu chopambana ndithu, koma tangoganizirani khamu limene lingamutsatire nthawi zonse kuti limuonetsetse. Nanganso nthawi yомуonera? Tikanatha ife kungokhala nayo mphindi yochepa basi kucheza naye m'moyo wathu wonse.

Yesu akufuna kukhazikitsa ubale weniweni ndi wina aliyense wa ife. Ichi ndi chimodzi mwa zifukwa zomwe lye anachoka kudziko lino lapansi pa utumiki wapadera kumwamba umene ungampange lye kudza chifupi nafe aliyense wa ife tsiku liri lonse. Popeza kuti Yesu siali malo amodzi okha ayi monga mmene zinaliri pamene anali m'dziko lapansi pano, mwa mzymu woyerera, ali paliponse kutsogolera munthu aliyense ndi moyo wake payekhapayekha, ngati munthuyo ali wofuna kutsogoleredwako.

Kodi ndi lonjezo la chilimbikitso lotani lomwe Yesu anapereka asanakwere kunka kumwamba?

"Ine ndiri pamodzi ndi inu masiku onse, kufikira chimaliziro cha nthawi ya pansi pano." - Mateyu 28:20.

Kodi kristu akuchita chiyani kumwamba chomwe chingapangitse kuti "akhale nanu masiku onse".

"Popeza tsono TIRI NAYE MKULU WA NSEMBE WOTHA kumva chifundo ndi zoooka zathu, koma woyesedwa m'zonse monga momwe ife, koma wopanda uchimo. Yesu mwana wa Mulungu Potero tilimbike mtima poyandikira mpando wachifumu wachisomo, kuti tilandire chifundo ndi kupeza chisomo cha kutithandiza nthawi yakusowa." - Aheberi 4:14-16.

Onani inu chitsimikizo cha chilimbikitso chotilonjeza kukhala naye Yesu ngati wotimirira wathu wathu kumwamba; "Woyesedwa munjira zonse, monga mmene ifenso tiriri". "Womva chisoni nafe mu zoooka zathu". "Wotithandiza mnthawi ya kusoweka kwathu", ndi Yesu monga mkulu wansembe, ife sitiri otsekeredwa kapena okhala kutali ndi kumwamba ayi.



Yesu atha kutilowetsa ife kumwamba pamaso pa Mulunguyo. Ndi chosadabwitsa kuti ife tikupemphedwa "kudza ku mpando wa chisomo molimba mtima".

Kodi Yesu akukhala malo ati kumwambako?

"Koma lye (Yesu), mmene adapereka nsembe imodzi chifukwa cha machimo, anakhala PA DZANJA LAMANJA LA MULUNGU," - Aheberi 10:12.

Khristu wamoyo - amene amamvetsetsa - ndiye wotii mira ku mpando wachifumu "kudzanja lamanja la Mulungu".

Kodi moyo wa Yesu udali bwanji kuti afike pokhala mkulu wathu wansembe?

"Potero kudamuyenera kufafanizidwa ndi ABALE mzonse, kuti akadzakhala mkulu wa ansembe wa chifundo ndi wokhulupirika mzinthu za kwa Mulungu, kuti apereke dipo la zoipa za anthu. Pakuti popeza adamva zowawa poyesedwa yekha, AKHOZA KUTHANDIZA iwo amene ayesedwa."
- Aheberi 2:17, 18.

"M'bale" wathu yemwe anagawana nafe umunthu wathu ndipo wakhala "woyesedwa" monga mmene ife tiri, ali wamkuru wathu wansembe kudzanja la manja la Mulungu. "Wopangidwa monga ife", amadziwa zonse zomwe tikukumana nazo. Iye anakhalaponso wanjala, waludzu, anayesedwa, namva kutopa. Anaona kufunka komveredwa chisoni ndikumvetsetsedwa.

Koma pamwamba pa zonsezi, Yesu anafikira pokhala wansembe wamkuru chifukwa anafa kuti apereke nsembe yotetezera "ku machimo athu. Analipira dipo lonse la machimo athu pofa m'malo mwathu, Uwu ndi uthenga wabwino kwa munthu aliyense, kulikonse ndi kunthawi iri yonse.

Mmodzi wa atsogoleri a masukulu athu ophunzirako za m'bukhu lopatulika akufuna kugawana nafe zomwe adakumana nazo motere: Pamene mwana wathu wamkazi wamng'ono adali ndi zaka zitatu, adapanitsa chala chake ku mpando nathyola fupa. Pamene tinathamangira naye kwa dotolo, kulira kwake kofuula ndi ululu kunadetsa nkhawa mitima yathu ndipo kunamukhuza mwapadera mwana wathu wina wa zaka zisanu. Ndipo sindikuiwala mau omwe adalankhula pamene dotolo adamaliza kumusamalira mbale wake wovulalayu. Mosisima adati. "Oh! Adadi, ndikadalakalaka chikadakhala chala changa!"

Pamene dziko lonse la anthu lidaphwasuka ndi uchimo ndi kuyenera kufa kwamuyaya, Yesu anati; "Oh, Atate, ndikulakalaka ndikadakhala Ine." Ndipo Atate anampatsa lye, Yesuyo, mongamwa kulakalaka kwake pa mtanda.

Mpulumutsi wathu waona zowawa zonse zomwe ife tikukumana nazo - ndiponso kuposerapo!

2. UTHENGA WA MU CHIPANGONO CHAKALE



Pamene ana a Israyeli adasonkhana mmensi mwa phiri la Sinayi, Mulungu adawalangiza kupyolera mwa Mose, kuti amange kachisi woyenda naye kuti adzipembedzeramo. "Motsatira momwe lye adawalangizira iwo kudzera mwa Mose, paphirilo la Sinayi" (Eksodo 25:40). Patangopita pafupifupi zaka Mazana asanu, Mfumu Solomon Adamanga kachisi wamkulu wolowa mmalo mwa kachisi wonyamulikayu. Ndipo kachisiyu adamangidwa motsatira ndondomeko yomweyo ya kachisi wamng'ono uja yemwe Mose adalangizidwa kumanga pa phiri la Sinayi.

Pamene Mulungu adampatsa Mose ndondomeko ija kamangidwe ka

kachisiyu, kodi iye adaona kufunika kwa mtundu wanji mumtima mwake?

"Ndipo andimangire malo opatulika, KUTI NDIKHALE PAKATI PAO." - Eksodo 25:8.

Uchimo udalekanitsa munthu ndi mlengi wake. Kachisi inali njira ya Mulungu yoonetsera mmene iye angalumikizaniranenso ndi kukhala nafe. Kachisi, kapena nyumba ya Yehova, inasandulika chilikati cha moyo wachipembedzo ndi matamando mu nthawi ya chipangano chakale. Mmawa uli wonse, anthu ankasonkhana mozugulira kachisi nalumikizana ndi Mulungu m'mapemphero (Luka 1:9, 10) kuitanitsa lonjezano la Mulungu: "Ndidzakumana nanu" (Eksodo 30:6).

Chipangano chakale tikuphunzitsidwa uthenga womwewo wa chipulumutso mmene ukupezekanso m'chipangano chatsopano. Zonsezi zikuonetsera Yesu wotifera ndi kutitumikira ife ngati wansembe wankuru mu kachisi wa kumwamba.

3. UTUMIKI WA YESU KWA IFE UNAONETSEDWA MKACHISI WA CHIPANGANO CHA KALE

Kachisi ndi atumiki ake onse amavumbulitsira ife zomwe Yesu akuchita panopa kumwamba mkachisi wa kumeneko; ndiponso zomwe akuchita panopa m'dziko lino lapansi kuti akatidzadza ndi kutitsogolera ife m'moyo wathu wa tsiku ndi tsiku.

Mu mitu ya 25 mpaka 40 ya bukhu la Eksodo, muli dongosolo la utumiki ndi miyambo ya kachisi wa mchipululu mwatsatanetsatane. Chidule chake cha kamangidwe ndi zopezeka mkachisimo chikuonetsedwa mu chipangano chatsopano.



"Ndipo lingakhale chipangano choyamba chinali nazo zoikika zakulambira, ndi malo opatulika apadziko lapansi.... M'menemo munali choikapo nyali, ndi gome, ndi mkate woonekera, apa panali pa malo opatulika. Koma mkati mwa chophimba chachiwiri, chihema chonenedwa malo opatulikitsa, okhala nayo mbale ya zofukiza ya golidi ndi likasa la chipangano, lokuta ponsepo ndi golidi momwemo munali mbiya ya golidi yosungamo mana. Mulikasamo munali.... Magome a miyala a chipangano (Pomwe Mulungu adalembapo Malamulo khumi (Denteronomo 10:1-5). Ndipamwamba pa che pa Likasa Akerubi a ulemerero akuchititsa mthunzi pachotetezerapo (mpando wachisomo)." - Aheberi 9:1-5.

Kachisiyu adali ndi zipinda ziwiri, malo opatulika ndi malo opatulikitsa. Kutsogolo kwa kachisiyi kunakonzedwa bwalo. Pabwaloli panali guwa la nsembe la mkuwa pomwe wansembe amaotchera nsembe, ndi mbiya yomwe amasambiramo m'manja.

Nsembe zoperekedwa pa guwa lamkuwali zimaimira Yesu, Yemwe kupylolera mu imfa yake ya pamtanda anasandulika. "Mwana wankhosa wa Mulungu, yemwe achotsa chimo lake la dziko lapansi" (Yohane 1:29) pamene wochimwa analapadi kusiya machimo ake paguwa amalandira chikhululukiro ndi chiyeretso. Mwa njira yomweyonso, wochimwa wa lero amalandira chikhululukiro ndi chiyeretso kupylolera m'mwazi wa Yesu (1 Yohane 1:9).

M' chipinda choyambachi, malo opatulika choikapo nyali zisanu ndi ziwiri mu nthambi zake zisanu ndi ziwiri zinali kuyaka nthawi zonse, kuonetsera kuti Yesu wosalepherayo "Kuunika kwa dziko lonse lapansi" (Yohane 8:12). Gome lokhala ndi mkate wopatulidwa limaimira Yesu wopezekeratu nthawi iri yonse pamene tiri ndi njala yauzimu, natikhutitsanso mu njala yathu yakuthupi. "Mkate



wamoyo" (Yohane 6:35).

Guwa la golidi la zonunkhira linaimira moyo wa Yesu wapemphero lakwa ife pamaso pa Mulungu mwini (Chibvumbulutso 8:3, 4).

Chipinda chachiwiri, malo opatulikitsa, munali likasa lachipangano lokuta ndi golidi. Iloli limaimira mpando wachifumu wa Mulungu chokhalirapo chaka cha chisomo, kapena chotetezera chimaimira mapemphero otetezera a Yesu, Wansembe wathu wamkuru, kupemphera mmalo mwa mtundu wa anthu wochimwa, omwe aswa malamulo a Mulungu a chikhwalidwe. Magome awiri a miyala pomwe padalembedwa malamulo khumi anali pansi pa mpando wachisomo. Akerubi a golidi aulemerero anzangulira mokuta mpandowu mmapeto aliwone a likasali. Nyali yowala mwaulemerero inaikidwa pakati pa Akerubi awiri, chizindikiro choti Mulungu mwini anali pomwepo.

Chinsalu chinaphimba malo opatulika kuti anthu asathe kuonako pamene wansembe anali kuwapempherera pabwalopo. Nsalu yachiwili inali kutsogolo kwa malo opatulikitsa kumphimbira kuti wansembeyu yemwe anali mchipinda choyambachi cha malo opatulika.

Pamene Yesu anafa pamtanda, chidachitika ndi chiyani ku nsaluyi?



"Ndipo onani chinsalu chochinga ca mkachisi chinang'ambika pakati, kuchokera kumwamba kufikira pansi," - Mateyu 27:51.

Malo opatulikitsa anaonekera pamene Yesu anafa. Itatha imfa ya Yesu, panalibenzo chochingira pakati pa Mulungu woyerwa ndi wokhulupirira moona, Yesu, wansembe wathu wamkuru, akutiitanira ife kwa Mulungu (Aheberi 10:19-22).

Tiri ndi mwayi ife wopita kumpando mchipindacho chachifumuncho kumwamba chifukwa choti Yesu ndiye wansembe wathu wankuru kudzanja lamanja la Mulungu. Yesu akutiyenereza ife kufika pamaso pa Mulungu ndi pa mtima wa chikondi wa Mulungu. Choncho "tiyeni tidze chifupi ndi lye".

4. CHIVUMBULUTSO CHA KHRISTU KUTIFERA KUTI TIPULUMUKE

Monga momwe kachisi woyambayo adali ngati nyumba ya Mulungu yaing'ono momwe Yesu anali kutumikira mmalo mwaife, Zochitika zake mmenemo zinali "Zofanana ndi Kapena chithunzithunzi cha zomwe ziri kumwamba" (Aheberi 8:5). Koma pali kusiyana kwina kwake koonekeratu: Ansembe omwe amatumikira mukachisimo samatha iwo kukhululukira chimo, koma pamtanda Yesu, "anaonekera kamodzi kokha nthawi yonse yadziko lapansi mkuchotseratu chimo kupolyera mu nsembe yodzipereka lye mwini" (Aheberi 9:26).

Chipangano chakale, m'bukhu la Levitiko, tikumva mwatsatanetsatane dongosolo la utumiki omwe umachitika mukachisiyo. Miyambo ndi maumutiki ake zinagawidwa pawiri. Utumiki wa tsiku ndi tsiku, ndi mwambo wa utumiki wa pachaka (monga tidzaphunzira mu phunziro lotsogolera la khumi ndi chitatu).

Mu utumiki watsiku ndi tsiku, wansembe amapereka nsembe ya munthu aliyense mumpingo wonse. Pamene munthu anachimwa, amabweretsa nyama yamoyo yopanda banga kapena chilema monga ngati chopereka kuti chimo likhulukidwe, "naika manja ake pamutu panyamayo ndikuiphera pa malo operekera nsembe" (Levitiko 4:29). Uchimo wa munthuyo umalowa mwa nyamayo yosalakwa ponena machimo ake otaika manja ake pa nyamayo. Izi zinaimira khristu wosenza machimo anthu onse pa Karivala, iye wosachimwa "nakhala chimo m'malo mwathu" (2 Akorinto 5:21). Nyama yansembeyo inayenera

kuphedwa ndi mwazi wake nukhetsedwa chifukwa zimalosera ku dipo lalikuru lomwe Khristu analizunzikira pa mtanda.

5. CHIFUKWA CHIYANI MWAZI?

"Popanda kukhetsa mwazi, palibe chikhululukiro" (Aheberi 9:22). Zomwe zinachitika mu kachisi wa m'chipangano chakale zimaonetsera Khristu ndi ntchito yake yopulumutsa. Atatha kutifera ife ku machimo athu, adalowa malo opatulika "kamodzi kokhako kokwanira ndi mwazi wake, atapeza chiombolo chosatha" cha ife (vesi 12). Pamene mwazi wa Yesu unakhetsedwa pa mtanda chifukwa cha machimo athu "Chinsaru cha mkachisi (Mu Yerusalem) chinang'ambika pakati kuyambira pamwamba mpaka pansi" (Mateyu 27:51) chifukwa cha Yesu kudzipereka nsembe pa mtanda, nsembe za nyama sizinali ndipo sizili zofunikanso ayi.



Pamene Yesu anakhetsa mwazi wake pamtanda, amapereka moyo wake wangwiro ndi womvera ngati cholowa m'malo mwa zolephera zathu. Pamene atate ndi mwana analakanitsidwa pa karivali, atate anatembenukira kumbali ndikumva kupweteka ndipo mwanayo anafa chifukwa chosweka mtima. Mulungu mwana analowa mu mbiri yodzitengera lye yekha mphoto yake ya uchimo ndi kuonetsera m'mene tchimo limaonongera. Tsono akanatha kukhululukira wochimwa aliyense mopanda kulichepetsa vuto la chimolo. Kristu anapanga " mtendere m'mwazi wake, wokhetsedwa pa mtanda" (Akolose 1:20).

6. BVUMBULUTSO LA YESU YEMWE ALIPO KUTIPULUMUTSA IFE

Kodi ntchito ya Yesu tsiku ndi tsiku ndiyotani mu kachisi wa kumwamba?

"Kuchokera komweko akhoza kupulumutsa konsekone iwo akuyandikira kwa Mulungu mwa lye, popeza ali nawo moyo wace chikhaliire wa kuwapembedzera iwo." - Aheberi 7:25.

Panopa Yesu "akukhala" kupereka moonetsera mwazi wake, nsembe yake, m'malo mwa ife. Panopa akugwira ntchito molimbika kupulumutsa munthu aliyense kuchoka ku tsoka lobwera ndi chimo. Anthu ena molakwitsa amaganiza kuti, Yesu, monga wotimira potipempherera, ali kumwamba kupempha Mulungu wosafuna kukhululukayo, kuti atikhululukire. Koma choti tidziwe ndi choti, ndi Mulungu yemweyo yemwe mokondwa analola kulandira nsembe ya mwana wake yochitikira chifukwa cha ife.

Monga wansembe wathu wamkuru, Yesu kumwambako, akudandaulira mtundu wa anthu. Akugwira ntchito yobweretsa maganizo ena a chisomo kwa anthu osiyana maganizo, komanso chiyemekezo kwa iwo amene akusowa chochita ndi zobvuta zamoyo, kupyolera onse kupeza chuma choposa mu mawu a Mulungu ndim'mphamvu ya pempher. Yesu akuiumbanso miyoyo yathu kuti igwirizane ndi Malamulo a Mulungu ndi kutithandiza kukula mu makhaliidwe athu kuti tikailandire imfa yake kuti ndiyo yachifukwa cha machimo athu.



Mulungu anataya moyo wake chifukwa cha munthu wina aliyense wokhala pa dziko lapansi. Ndipo panopa, monga wansembe wamkuru ndi m'khalaapati, "alipo nthawi zonse" kutitsogolera ife anthu ake kuti tikailandire imfa yake kuti ndiyo yachifukwa cha machimo athu.

Ngakhale anayesetsa kuliyanjanitsano dziko lapansi lakugwalo ku chiyanjano chatsopano ndi lye pamtanda, sangathebe kutipulumutsa pokhapokha titalandira ndi kuvomereza chisomo chake. Anthu

sadzataika chifukwa choti iwo ndi wochimwa ayi, koma chifukwa chakuti akana kuvomereza chikhululukiro chamachimo chimene Yesu waperekwa.

Chimo lidaononga ubale weniweni womwe udalipo pakati pa Adamu ndi Hava ndi Mulungu wawo, womwe amasangalala nawo. Koma Yesu, monga mwana wa nkhsosa wa Mulungu, anafera mtundu wonse, kumchotsa ku chimo mwaulere; ndi kubwezeranso ubale uwo womwe udasokonezekawo. Kodi inunso mwapeza kuti lye ali mkulu wanu wansembe, amene akhala ku nthawi zonse kubweretsa ubalewo pafupi ndi kumpanga weniweni?

Imfa yodzipereka nsembe ya Khristu ndi yapayokha. Utumiki wa Yesu Khristu kumwamba ndiyosayerekezeka ndi china chilichonse. Ndi Khristu yekha yemwe amamubweretsa Mulungu pafupi pathu. Ndi Khristu yekha amene amapanga zotheka kuti mzimu woyerwa wopatulika akhala m'mitima yathu. Anadzikhuthula lye ngati wopanda kanthu kuti ife tikakhale athunthu. Iyenso akuyenera kuti ife tikadzipereke kwa lye chomwecho. Tiyen'i timulandire kwanthunthu lye ngati Mpulumutsi ndi mbuye wa miyoyo yathu.

KUCHOKERA KU KUTSUTSIKA NDI CHIMO KUFIKIRA KU WOYERA WOKHULULUKIDWA

Sadapeza malo pomwe panagwira zala. Palibenso chida chomwe chidapezeka. Wakuphanso sanaoneke akusowa mu ofesi ya dotoloyo. Palibenso adamva kulira kwa mfuti. Koma kunapezeka kuti dotolo ali gone pa mpando wake wa muofesi. Zipolopolo za mfuti zisanu zikuonekera kuti zaboola malaya ake ndikulowa m'thupi.

Zinaoneka ngati chinali chiwembu changwiro. Apolisi sanathe kupeza umboni uliwonse pachiyambi koma adapeza waya wina wake wan'gono atamangiliridwa ku nsonga ya choikamo pensulo pa tebulo lantchito la dotoloyo. Wayayo adakafikira ku wailesi yojambula mau yomwe inali muchosungira zinthu chapatebuloyo. Anazindikira kuti, choikamo pensulocho, chinali chitaphimbira chija choyankhulirapo mawu, (microphone) chomwe dotolo ankagwiritsa pojambula zokambirana ndi odwala ake amene anayenera kuwapatsa malangizo.



Ofufuza adaibweza tepi yojambulidwayo, ndipo anadabwa, pamene anamvetsera tepiyo kupeza kuti imakamba zokhudzana ndi chiwembu chomwe chidapha dotoloyo. Mwamuna wotchedwa Anthony adalowa mu ofesiyo nayamba mkangano waukuru ndi dotoloyo. Kenaka kunamveka kulira kwa mfuti ndipo tepiyo inathera ndi kulira kosautsika ndi ululu kwa dotoloyo, akufa kugwera pa nsalu ya muofesiyo.

Choopsa chirichonse chinajambulika. Wakuphayo amaganiza kuti chiwembucho sichidzaululikanso. Anayesetsa kuchita mosamala kuti pasapezeke umboni uliwonse. Koma tepiyo idapereka umboni wonse.

Muchotsogolera cha phunziro ili, tiphunzira za chiweruzo chomaliza cha Mulungu pamene anthu adzaweruzidwa "malinga ndi zomwe iwo adachita, zomwe zalembedwa m'mabukhu" (cibvumbulutso 20:12) kwa; iwo amene sanamulandire khristu ngati Mpulumutsi wawo; kwaiwo kudzakhala nkhanji yoipa. Koma chiweruzochi chidzakhala nkhanji yabwino kwa iwo amene anapeza kupuma mwa khristu.

1. M'MENE MUNGAFIKIRE KUCHIWERUZO MOPANDA MANTHA

Kodi adzaweruza dziko lapansi ndani?

"Pakuti Atate saweruza munthu aliyense, koma anapereka kuweruza konse kwa Mwana." - Yohane 5:22.

Kodi nanga mtanda unamkonzetsera bwanji Yesu Khristu kuti akhale woweruza wathu?

"Amene Mulungu anaunika poyer (Yesu) akhale cotetezera mwa cikhulupiriro cam'mwazi wace, kuti aonetsera cilungamo cace... kuti lye akhale WOLUNGAMA, NDI WAKUMUYESA WOLUNGAMA lye amene akhulupirira Yesu," - Aroma 3:25, 26.



Imfa ya khristu m'malo mwa ife inapangitsa lye kukhala yekha woweruza komanso wotilungamitsa yemwe angathe kutikhululukira ife tikalapa machimo athu. Pamene dziko lapansili likuonerera zochitika zake ndikhala ndi mafunso ngati awa, "kodi woweruza angathenso bwanji kumupanga wolakwayo kukhala wopanda mlandu?" Khristu atha

kuyankha poonetsa zipsera za mabala m'manja mwake,. Analandira dipo lakuyeretsera machimo athu m'thupi lake mwini.

Mabukhu a kumwamba amasungira zochitika zonse za m'moyo wamunthu aliyense, ndipo zochitika zosungidwazo zimagwiritsidwa ntchito pa chiweruziro (Cibvumbulutso 20:12).

Iyi ndi nkhani yowawa kwa iwo omwe amaganiza kuti machimo awo amtseri ndi ziwembu zawo sizidzawapezanso. Koma pali nkhani yabwino yokoma kwa iwo omwe adadzichepetsa kumlandira khristu ngati wowaimirira pa mlandu wawo kumwamba: "mwazi wa Yesu... utiyeretsa ife kumachimo athu" (1 Yohane 1:7).

Kodi Yesu amausinhanitsa moyo wathu wa uchimo ndi chiyani?

"Ameneyo sanadziwa ucimo anamyesera ucimo m'malo mwathu kuti ife tikhale cilungamo ca Mulungu mwa lye." - 2 Akorinto 5:21.

Moyo wathu wa uchimo umasinhanitsidwa ndi moyo wangwiyo wachilungamo wa khristu chifukwa chakufa kwa Yesu wosachimwa, Mulungu atha kutikhulukira ife ndikutitenga monga ngati sitidachimweko cikhaliire. Kodi chamuyenera Yesu kukhala wotimira ndi wotiweruza pa mlandu wathu ndi chiyani?

2. YESU ANABWERA PANTHAWI YAKE

Pa ubatizo wake, Yesu anazunzidwa ndi mzimu woyeria.

"Ndipo Yesu pamene anabatizidwa , pomwepo anaturuka m'madzi: ndipo onani, miyamba inatsegukira lye, ndipo anapenya mzimu wa Mulungu wakutsika ngati nkhunda nudza nutera pa lye: ndipo onani, mau akucokera kumiyamba akuti "Uyu ndiye mwana wanga wokondedwa, mwa iyeyu ndikondwera." - Mateyu 3:16, 17.

Potsatira bwino kudzodzedwa kwa Yesu ndi Mzimu woyeria pa ubatizo wake, ophunzira ake analengeza:

"Tapeza ife Mesaya" (ndiko kusandulika Kristu)."- Yohane 1:41.

Ophunzirawa ankadziwa liwu lachiHebri loti "Mesiya" ndi lina lachiherene loti "khristu" onsewa atanthauza "amene ali wodzozedwa."

Wophunzira wina wa Yesu dzina lake Luka, analemba zatsiku lomwe Yesu anadzozedwa ngati Mesiya kuti chinali chaka chachisanu kulamulira kwa Kaisara. Tiberiyu (Luka 3:1) kwa ife nthawi imeneyo idali chaka cha A.D. 27.

Kupyolera zaka mazana asanu Yesu asanabwere, m'neneri Danieli analosera kuti Yesu adzadzozedwa monga Mesiya m'chaka cha A.D.27.

"kuyambira kuturuka lamulo lakukonzanso, ndi kumanga Yerusalem, kufikira wodzozedwayo... kudzakhala masabata makumi asanu ndi limodzi mphambu ziwiri makwalala ndi chemba zidzamangidwanso." - Daniel 9:25.

Masabata asanu ndi awiri ndi masabata makumi asanu ndi chimodzi mphambu ziwiri, zonsezi pamodzi zitipatsa masabata makumi asanu ndi limodzi mphambu zisanu ndi zinayi, kapena masiku mazana anayi makumi asanu ndi atatu ndi mphambu zitatu (483 days).



Muzizindikiro za m'baibulo ndi ulosi wake, tsiku limodzi limaimira chaka chimodzi (Ezekiel 4:6, Numeri 14:34), ndiyeno masiku tachulawo akuimira zaka mazana anayi makumi asanu ndi atatu mphambu zitatu (483 years).

Danieli adalosera kuti ulamuliro udzaperekedwa kubwezera ndi kumanganso Yerusalem, ndipo patapita zaka zimene tatchulazi chiikire ulamuliro Mesiya adzaonekera.

Kodi Yesu adaonekera ngati Mesiya nthawi yoikikayi? Aritasasta, mfumu adapereka lamulo kumanganso Yerusalem m'chaka cha 457 B.C. (Ezara 7:7-26). Ndipo zaka izi mazana anayi makumi asanu ndi atatu mphambu zitatu zinathera m'chaka cha A.D. 27 (457 B.C + A.D. 27 = 484). Lamuloli lidapitirirabe m'chaka cha 457 ndipo khristu anadzodzedwa m'nthawiyi ya chaka cha A.D.27, kupangitsa zakazi kukhala mbali imodzi kuti nthawi yake yeniyeni ikakhale zaka mazana anayi makumi asanu ndi atatu mphambu zitatu.)

Munthawi yake yoikikayo, m'chaka cha A.D. 27, Yesu anaonekera ndi uthenga: "nthawi yafika" (Marico 1:15). Kukwaniritsidwa kwenikweni kwa ulosi wa m'baibulo ndi kokwanira kutsimikizira kuti Yesu waku nazareti ndiyedi Mesiya, Mulungu muthupi la umunthu.

Kodi panayenera kutenga nthawi yaitali bwanji kuti Yesu akwaniritse lonjezo?

"Ndipo adzapangana cipangano colimba (lonjezo) ndi ambiri sabata limodzi." - Danieli 9:27, mbali yoyambirira.

Tikatengera chiwerengero cha tsiku kuimira chaka, "sabata" iyi ikhala zaka zisanu ndi ziwiri. Ndiye kwazaka zisanu ndi ziwiri-kuyambira m'chaka cha A.D. 27 kufikira A.D. 34. Yesu akada "kwaniritsa chipangano, "kapena lonjezo lomwe adapanga kwa Adamu ndi Hava atangochimwa. Mulungu adapanga pangano, lonjezano, kuti adayenera kupulumutsa mtundu wa anthu kuchokera ku tchimo kupyolera mu imfa ya wina wake yemwe akadamtuma kudzafera machimo athu (Genesis 3:15).

Chinayenera kuchitika n'chiyani mkatikati mwa sabata ya makumi asanu ndi awiriyi?

"Ndi pakati pa sabata adzaleketsa nsembe yophera ndi nsembe ya ufa." - Daniel 9:27.



Yesu anapachikidwa m'chaka cha A.D. 31 "mkatikati mwa sabatayi" pa nthawi yomwe khristu anafa, Mulungu "anang'amba nsaru ya m'kachisi... pakati kuyambira kumwamba mpaka pansi (Mateyu) 27:51). Nsembe yopsereza yoperekedwa kuti iphedwe (yoimira Yesu "Mwana wa nkosa wa Mulungu" idathawa m'manja mwa wansembe. Ichi chiniali chizindikiro kuti Mulungu safunanso munthu kuti adzipereka nsembe ya nyama. Uku kukwaniritsa ulosi wakuti Yesu "anathetsa" kufunika kumaperekabe nsembe yodzera muimfa ya Yesu, anthu akupezeramo mwai wofika kwa Mulungu mowaperekanso nsembe kupyolera mwa akuru ansembe, koma kupyolera mwa Mesiya, mwana wa nkosa wa Mulungu.

3. CHITSIMIKIZO KUTI MACHIMO AKHULULUKIDWA

Monga mwa ulosi wa Danieli, ndi chifukwa chiyani Yesu anafa?

"Wokozedwayo adzalikhidwa, nadzakhala wopanda kanthu."
- Danieli 9:26.

Paimfa yake pamtanda, Yesu "analekanitsa." Anafa, "osati kudzifera yekha" osatinso kulipira dipo la tchimo lake, koma kulipira dipo la machimo a dziko lonse lapansi kodi tingadziwe bwanji kuti Mulungu wakhulukira machimo athu?

"Ndipo cilungamo ca Mulungu cimene cicokera mwa cikhulupiriro capa Yesu Khristu kwa onse amene akhulupirira... pakuti ONSE ANACHIMWA..., ndipo ayesedwa olungama kwaulere, ndi cisomo cace, mwa ciombolo ca mwa khristu Yesu... mwa cikhulupiriro ca mwazi wace." - Aroma 3:22-25.

Mfundu zenizeni mu mavesiwa ndi awa: Ife "tonse tinachimwa," koma cifukwa cha chisomo cha Mulungu, tonse "tidalungamitsidwa" amene ali "ndi chikhulupiriro" mu mphamu yakuyeretsa ya "Mwazi" wa khristu. Pamene tilungamitsidwa, Mulungu amaticha ife wopanda tchimo, nafafaniza mphulupulu zathu zonse zakale. Ndipo amatitcha ife wolungama, "chilungamo cha kwa Mulungu chichokera mu chikhulupiriro cha mwa Yesu Khristu."



Tonse amene tatunduzidwa pofuna kuyesetsa kukhala wolungama mwatokha, titha kupeza mpumulo weniweni mu chisomo chakutilandira cha khristu. Akutilonjeza kuti, "idzani kwa lne, inu nonse akulema ndi akuthodwa, ndipo ndidzakupumulitsani" (Mateyu 11:28). Tonse amene talemedwa ndi zipsera za ukali wathu ndikumva kuperewera kwathu ndi manyazi, titha kupeza mtendere ndi umphumbu mwa khristu.

4. NTHAWI YA CHIWERUZIRO KUFUNA KUYAMBIKA

Mu mutu wakhumi ndi chisanu ndi chitatu cha Danieli muli m'ngelo yemwe akuonetsa Daniel zinthu zazikuru zodzachitika kutsogolo. Daniel adaona:

(1) Nkhosa yamphongo, (2) mbuzi yamphongo ndi (3) nyanga imodzi yomwe mbuzi yamphongoyi idali nayo " munatuluka nyanga ina yomwe inayamba ngati yaing'ono, naikula mu mphamu" (Daniel 8:1-12, 20:26).

Kodi mbali yachinayi ya ulosiwu ndi yotani?

"Masomphenya a nsembe yopsereza yachikhaliire, ndi cholakwa chakupulumutsa ca kupereka malo opatulika ndi khamulo ziponderezew, adzakhala mpaka liti? Nati kwa ine, mpaka masiku zikwi ziwiri mphambu mazana atatu usana ndi usiku; pameneo malo opatulika adzayedewa olungama." - Daniel 8:13, 14.

Daniel adakomoka m'ngelo asadayambe kulongsola za mbali ya masiku zikwi ziwiri mphambu mazana atatu ya ulosi, ndipo mutu wachisanu ndi chitatu ukutha usanamasulire ulosiwu. Koma nthawi inanso mngeloyu anabweranso nanena:

"Ndaturuka tsopano ine kukuzindikiritsa mwa luntha. Pakuyamba iwe mapembedzero ako, linaturuka lamulo, ndipo ndadza ine kukufotokozena. Masabata makumi asanu ndi awiri olamulidwira anthu a mtundu wako ndi mudzi wako wopatulika, kumariza colakwa, ndi kutetezera mphulupulu." - Daniel 9:22-24.

Masiku zikwi ziwiri mphambu mazana atatu, indedi ndi zaka zimenezo, tsiku limodzi liimira chaka chimodzi (Ezekiel 4:6). Masabata makumi asanu ndi awiri, kapena masiku mazana anayi mphambu makumi asanu ndi anayi, ziri mbali imodzi yaitali kwambiri yoyambirira ya Zaka zikwi ziwiri mphambu mazana atatu. Nthawi zonzezi zinayamba m'chaka cha 457BC pamene Perezi adapereka lamulo "lobwezera ndi kumanganso Yerusalem." Kuchotsera zaka zobwezera ndi kumanganso Yerusalem. Kuchotsera zaka mazana anayi mphambu makumi asanu ndi anayi ku zaka izi zikwi ziwiri mphambu mazana atatu, titsala ndi chikwi chimodzi, mphambu mazana asanu ndi zitatu ndikhumi kuphatikizira zaka zotsalazi ku chaka cha A.D. 34, pamene zaka mazana anayi mphambu makuni asanu ndi anayi zidathera, zikutipatsa chaka cha A.D. 1844.

5. KUYERETSEDWA KWA KACHISI WA KUMWAMBA- CHIWERUZIRO

Mngelo adamuuza Daniel kuti m'chaka cha 1844, kumapeto kwa zaka zikwi ziwiri mphambu makumi atatu, "kachisi adzayeretsedwa" (Daniel 8:14). Koma nanga izi zikutanthauza chiyani? Kuyambira m'chaka cha A.D. 70 pamene Aroma adaononga kachisi wa Yerusalem, anthu a Mulungu adakhala opanda kachisi pa dziko lapansi. Kachisi woti ayeretsedwe, kuyambira mu 1844, anayenera kukhala wakumwamba yemwe amafanana ndi yemwe adali pansi pano.



Nanga, zitanthauzanji kuyeretsa kachisi wakumwamba? Israeli wakale ankalitcha tsiku loyeretsa kachisi wa pansi pano kuti yomu kipuru, tsiku lachitetezero. Linalidi tsiku la chiweruziro.

Monga mmene tidaonera mu phunziro lakhumi ndi chiwiri lija, ntchito yakhrusu kwa ife mu kachisi yagawidwa pawiri:
 (1) Nsembe yatsiku ndi tsiku imaonetsera utumiki wa wansembe muchipinda choyamba cha kachisiyo, malo opatulika.

(2) Nsembe ya pachaka imaonetsera ntchito yapamwamba ya utumiki wa unsembe m'chipinda chachiwiri, malo opatulikitsa (Revitiko 16).

Mukachisi wa dziko lapansi, pamene anthu ankalapa machimo awo tsiku ndi tsiku, mwazi wa nyama yophedwa umawazidwa pambali pamapeto a guwa lansembe, ndipo umasamutsidwa ku malo opatulika (Levitiko 4 ndi 6). Kusonyeza kuti, mzoimirira, tipeza kuti tsiku ndi tsiku, machimo amaperekedwa ku kachisi kudasiidwa kumeneko anthu okalapa.

Ndipo chaka chiri chonse, pa tsiku lachitetezero, kachisi amayeretsedwa kumachimo onse olapidwa chaka chonse (Levitiko 16). Kuti kuyeretsa uku kutheke, mkulu wansembe amaperekwa nsembe yapadera ya mbuzi yopanda banga yopatulidwa. Ndipo mwazi wa mbuziyo amautenga kukalowa nawo ku chipinda chopatulikitsa nawaza mwaziwu pa chofundira cha chitetezero kuchipindako kusonyeza kuti mwazi wa Yesu, mombolo alikudzayo, adzalipira dipa la zochimwa zonse. Wamkuru wansembeyu woyerekezera amakhala ngati wachotsa machimo onse omwe anthu adalapa mkachisimo kuwatula pa mutu pa mbuzi ina, yomwe imasiyidwa kupita kuchipululu kuti ikafe (Levitiko 16:20:22).



Mwambo uwu wachitetezero wa tsiku lapachaka umayeretsa kachisi ku tchimo. Anthu ankalitenga tsikuli ngati lachiweruziro, chifukwa omwe adakana kulapa machimo awo amatchedwa wosayera ndipo "amachotsedwa m'gulu la anthu a Mulungu" (23:29).

Chomwe anayerekeza wansembe dziko lonse lapansi (cibvumbulutso 14:6-7). Mtsogolomu, m'maphunziro athu omwewa tidzaphunzira za uthenga umenewu.

6. KUDZAPEZANA NDI ZOMWE MUNACHITA M'MOYO PA CHIWERUZIRO

Kuyambira mu 1844, Khristu, monga woweruza, wakhala akufufuza mu 1844, khristu, monga woweruza, wakhala akufufuza mabukhu a munthu aliyense wokhala pa dziko lapansi kuti otsimikizira za iwo amene ali woyeru kukakhala opulumutsidwa pamene Yesu adzabwera. Monga woweruza wathu, Yesu "akufufuta" machimo onse a anthu oyera kuchokera mu mabuku awo a moyo kumwamba (Macitidwe 3:19).



Dzina lanu likadzafika pachiweruziro, zidzakhala zosavuta kukumana ndi ntchito zathu zomwe zinalembedwa-koma pokhapokha ngati mwamulandira Yesu khristu monga wolowa m'malo wanu, ndipo pamene chiweruziro cha olungama chatha, Yesu adzabwerera ku dziko lapansi kudzapereka mphotho kwa iwo (Cibvumbulutso 22:12,14).

Kodi inu mwakonzekera kubwera kwa Yesu? Kapena pali china chake chomwe mwakhala mukumubisira lye? Kodi muli pa ubale woongoka ndi woona womasuka ndi yemwe walonjeza kuti:

"Ngati tibvomereza macimo athu, ali wokhulupirika ndi wolungama lye, kuti atikhululukire machimo athu, ndikutisambitsa koticotsira cosalungama ciri conse." - 1 Yohane 1:9.

Kulapa kutanthauza mosavuta kuti tavomera kukumana ndi machimo athu, ndi kuvomereza chikhululukiro cha Mulungu komanso kuzindikira kufunika kwa mphamvu yake ndi chisomo chake kwa ife.

Mfumu ina yotchedwa Fredrick William woyamba adamvetsera madandaulo a kufuna chikhululukiro kundende ina yomwe adakachezako ya ku Potsdam. Am'ndende onse adalumbira nati oweruza okondera, mboni zonama, ndi oyimirira milandu yawo osadziwa ntchito, adachititsa kuti iwowa apezeke mundende chomwechi. Kuchokera chipinda china chandende kufikira china, onse ankanena chimodzimodzi mopitiriza kuonetsa kuti anali wosachimwa.

Koma m'chipinda china wandende mmodzi adalibe chonena. Modabwitsika, Fredrick adaseleula motere naye, "ndiyesa inunso ndinu wosalakwa."

"Ayi mfumu yanga," munthuyo adayankha, "ine ndine wolakwa ndithu ndipo chilangochi ndichondiyenera." Ndipo mfumu idatembukira kwa woyang'anira m'ndende naitana mofuula, "Idzani ndi kumtulutsa munthuyu mwachangu, asanafike poononga gulu la anthu osalakwali."

Kodi ife timakonzekera bwanji chiweruziro? nanga timamukonzekera bwanji Yesu khristu pakubwera kwache? Pongolapa moona mtima wachikhulupiriro kunena kuti: Inedi ndiyenera dipa la imfa chifukwa cha machimo anga, koma wina walowa m'malo mwanga ndikundipatsa ine chikhululukiro chozizwitsa.

Pangani chitsimikizo tsopano ndi kunena kuti kaya zivute bwanji kaya, mudzasunga ubale wanu maso ndi maso ndi Yesu kuti ukakhale woona wa pansidi pamtima.

CHINSINSI CHA PEMPHERO LOYANKHIDWA



Wolemba wina wa ku Russia, dzina lake Anatoli Levitin, yemwenso ali katswiri pa mbiri, anakhala zaka zambiri ku Gulag wa ku Siberia kumene kukhulupirira mwa Mulungu kudazizira mpaka kutsikiratu. Koma adabwerako ali wodzala ndi uzimu. "chozizwa cha zonse ndicho pemphero," lye adalemba motero. "ndiyenera kutembenkira kwa Mulungu m'maganizo ndipo kamodzi komweko ndikumva mphamvu yachikakamizo yotsanulidwira mwa ine kuchokera kwina kwake, kudza mumtima mwanga, ndi mthupi langa lonse.

Kodi nanga ichi nchiyani? Nanga ine wokalamba, wotopa ndi moyo ndi wopanda pake ine, ndikakhala kuti ndi kupeza mphamvu yondikweza ine pamwamba padzikola lapansi? Izi zichokera kunja kwa ine - ndipo palibe mphamvu m'dziko lapansi yomwe ingaletse izi.

Mu phunziro iri, tiona mmene pemphero limathandizira kumanga ubale wamphamvu ndi Mulungu ndi moyo wachikhristu wangwiyo.

1. KULANKHULANA NDI MULUNGU

Kodi tingakhale bwanji ndi chitsimikizo kuti Mulungu amamva mapemphero athu?

"Pamenepo mudzandiitana Ine, ndipo mudzanka ndikupemphera kwa Ine, ndipo ndidzakumverani inu." - Yeremiya 29:12, 13.

Kodi ndi chitsimikizo chiti chomwe Yesu adapereka choti adzamva ndi kuyankha mapemphero athu?

"Ndipo Ine ndinena ndi inu, pempani ndipo adzakupatsani, funani, ndipo mudzapeza, gogodani ndipo adzakutsegulirani." - Luka 11:9.


Pemphero ndi kukambirana kwa mbali ziwiri. Izi ndi zomwe Yesu alonjeza.

"Taona, ndaima pakhomo, ndigogoda; wina akamva mau anga nakatsegula pakhomo, ndidzalowa kwa iye, ndipo ndidzadya naye, ndi iye ndi Ine." - Cibvumbulutso 3:20.

Kodi ndizotheka bwanji kukhala ndi mgonero wazokambirana ndi khristu? Choyamba, pomuuza zonse zamumtima mwathu kupolyera mu pemphero. Chachiwiri, pomvera mosamalitsa pamene tipemphera, Mulungu atha kuyankhula nafe chindunji pamene tiwerenga mawu a Mulungu modziperekira, Mulungu adzayankhula nafe m'mawuwo. Pemphero litha kukhala njira yamoyo kwa Mkristu.

"Kondwerani nthawi zonse PEMPERANI KOSALEKA; m'zonse yamikani; pakuti ici ndi chifuniro ca Mulungu ca kwa inu, mwa Khristu Yesu." - Atesalonika 5:16-18.

Kodi "tingapemphere bwanji kosalekeza"? Kodi ife tikhale chigwadire nthawi zonse ndi kubwerezabwereza polankhula mapemphero athu ndi zofuna zathu? Sichoncho ayi. Koma tiyenera kukhala pafupifupi ndi



Yesu kuti tikhale aufulu kuyankhula naye nthawi iriyonse paliponse.

"Kaya tiri pakati pa anthu ambiri mumsewu, pakati pa ntchito yamalonda, titha kupereka nkhwawa zathu kwa Mulungu ndi kupempha chitsogozo chakumwamba... khomo lamtima wathu liyenera kukhala lotsegula nthawi zonse ndi kuitana Yesu kuti adze kudzakhala ngati mlendo wakumwamba mmoyo wathu-mapazi opita kwa khristu, tsamba 99.

"Pomlingirira lye pandikonde; ndidzakondwera mwa Yehova." - Masalmo 104:34.

Popemphera sitiyanera ife kungofikira kuyala m'ndondomeko wazosowa zathu ayi. Dikirani, mvetserani pemphero lalifupi lakudzipereka litha kukuza ubale wanu ndi Mulungu.

"Yandikirani kwa Mulungu, ndipo adzayandikira kwa inu." - Yakobo 4:8.

Pamene tiyandikira kwa Yesu, ndipamenenso tinatha kumva kuti ali pakati pathu. Ndiye tiyeni tikhale paupipafupi poti tingayankhule naye Yesu, ndipo tisadandaule ndi kuti mawu amene timiuza ndi oyenera kapena ayi. Timiuza chirichonse moona ndi mosasuka. Iye wadutsamo kale muchizunzo cha imfa yeniyeni ndi cholinga choti akakhale bwenzi lathu lenileni.

2. MMENE TINGAPEMPHERERE

Tikamapemphera, titha kusankha kutsatira ndondomeko ya pemphero la Ambuye, lomwe iye adaphunzitsa akuphunzira ake atamupempha kuti "Tipunzitseni mmene tingapempherere."

"Atate wathu wakumwamba, Dzina lanu liyeretsedwe. Ufumu wanu udze. Kufuna kwanu kucitidwe, monga kumwamba comweco pansipano. Mutipatse ife lero cakudya cathu calero. Ndipo mutikhululukire mangawa athu, monga ifenso takhulukira amangawa athu. ndipo musatitengere kokatiyesa, koma mutipulumutse kwa woipayo. pakuti wanu ndi ufumu ndi mphamvu ndi ulemerero wa nthawi zonse, Amen." - Mateyu 6:9-13.



Potsata ndondomeko ya pemphero yomwe Yesu anapereka mupemphero lake, tiyenera ife kudza kwa Mulungu monga Atate wathu. Tipemphe kuti kufuna kwake kokha ndiko kuchitike m'mitima yathu monga mmene zichtikiranso kumwamba.

Timamufuna iye kuzosowa zathu zakuthupi, kuchikhulukiro, ndi mtima wokhululukira. Kumbukirani kuti, ife tithe kupewa tchimo, Mulungu ndiye angatithandize. Pemphero la Khristu likutha ndi chiyamiko kapena matamando.

Munthawi inanso, Yesu adawalangiza ophunzira ake kupemphera kwa Atate "m'dzina lake." (Yohane 16:23) kutanthauza kuti, azipemphera mogwirizana ndi ndondomeko ya Yesu. Ndichifukwa chake akhristu ayenera kutseka mapemphero awo ndi mawu awa: "m'dzina la Yesu, Amen" liwu loti "Amen" litanthauza kuti "zikhale chomwecho." muchiHeberi.

Ngakhale pemphero la Ambuye likutitsogolera pa zoyenera kupempha ndi m'mene liyenera kukhalira pempherolo, kulumikizana kwathu ndi Mulungu kumapambana ngati zopempha zathu zikuchokera pansi pamtima.

Titha kupempherera chirichonse. Komanso Mulungu akutitianira ku kupempherera chikhululukiro cha macimo athu; (1 Yohane 1:9), kuchulukitsidwa kwa chikhulupiriro (Mariko 9:24), zofunika za m'moyo

(Mateyu 6:11), Machiritso ku zowawa ndi matenda (Yakobo 5:15), ndi kuvumbitsidwa kwa mzimu woyerwa (Zekariya 10:1). Yesu akutitsimikizira ife kuti titha kutengera zosowa ndi nkhawa zathu kwa lye: Palibe chomwe chiri chochepa kuchipempherera.

"Ndikutaya pa lye nkhawa yanu yonse, pakuti lye asamalira inu." - 1 Petro 5:7.

Mpulumutsi wathu anakondweretsedwa mu chiri chonse cha m'moyo wathu. Mtima wake umafunda pamene mtima wathu ufikira kwa lye m'chikondi ndi chikhulupiriro.

3. PEMPHERO LAMTSERI



Ambiri aife tiri ndi zinthu zina zomwe sitingamasuke kuza ngakhale abwenzi athu apamtimia. Chotero Mulungu akutiitanira ife kuti timumasulire ife tokha izi mu pemphero lathu lamtseri: inu ndi iyeyo basi. Sikuti akufuna kupezapo nkhani yanuyo ayi. Mulungu wamphamu zonezi amadziwa zinsinsi zathu, zotiopsa zathu, malingaliro athu obisika, ndi zokwiririka zathu zomwe tazichita koposa m'mene ife eni ake tikudziwira. Koma tiyenera tiyambe tamasuka naye lye wodziwa zonezi ndi kumutsegulira mitima yathu, popeza lye wotikondayo amatidziwa chiyambi mpaka mapeto athu. Kuchira kungayambike ndi kukhuza kwa Yesu ku mabala athu. Pamene tipemphera, Yesu, wansembe wathu wamkuru, ali pafupi kuti atithandize:

"Pakuti sitiri naye mkuru wa ansembe wosatha kumva cifundo ndi zofoka zathu; koma woyesedwa m'zonse monga momwe ife, koma wopanda ucimo. Potero tilimbike mtima poyandikira mpando wacifumu wacisomo, kuti tilandire cifundo ndi kupeza cisomo ca kutithandiza nthawi yakusowa." - Ahebri 4:15, 16.

Kodi mumachita mantha, kupsinjidwa ndi kumva kuti muli wolakwa? Zonezi zituleni pamaso pa Ambuye. Ndipo adzatipatsa chosowa chathu chiri chonse.

Kodi tiyenera ife kukhala ndi malo apadera ochitira mapemphero athu amtseri?

"Koma iwe popemphera, Iowa m'chipinda cako, utseke citseko cako, nupemphere Atate wako ali mtseri... ndipo adzakubwezera iwe." - Mateyu 6:6.

Tithango kupemphera moonjezera pamene tikuyenda pa msewu, pamene tikugwira ntchito, pamene tiri pachisangalalo ndi anzathu; Mkhristu aliyense apeze kanthawi tsiku lirilonse kopemphera payekha ndi kuwerenga Bukhu lopatulika. Lumikizanani ndi Mulungu tsiku ndi tsiku munthawi imene mukuona kuti muli tcheru ndipo mutha kumvana bwino naye.

4. PEMPHERO LA PAGULU



Kulumikizana ndi ena m'mapemphero kumabweretsa ubale wina wake wapadera ndi kuitanitsa mphamu ya Mulungu mwa njiranso yapadera.

"Pakuti kumene kuli awiri kapena atatu asonkhanira m'dzina langa, ndiri komweko pakati pao." - Mateyu 18:20.

China mwa zinthu zoposa chomwe tingathe kuchita ngati banja ndicho kukuza moyo wathu wakupempherera pamodzi. Onetsani ana anu kuti titha kupereka zosowa zathu mwachindunji kwa lye. Iwo adzasangalatsidwa ndi Mulungu poona kuti mapemphero

akuyankhidwa ndi lye moonekeratu m'moyo. Pangani mapemphero a m'banja kukhala wosangalatsa ndi kukhala nthawi yakugawana momasuka.

5. ZINSINSI ZISANU NDI ZIWIRI ZAKUYANKHIDWA KWA PEMPHERO

Pamene Mose adapemphera, panyanja yofiira, madzi anagawanika. Pamene Eliya adapemphera, moto unatsika kuchokera kumwamba. Pamene Danieli anapemphera, mngelo wa Mulungu adatseka pakamwa pa Mikango yolusa. Bukhu lopatulika likutionetsera ife ndi zitsanzo zosangalatsa zambiri za kuyankhidwa kwa mapemphero. Ndipo likuchitira umboni kuti pemphero ndi njira yotsitsira mphamvu za Mulungu zazikulu kuti zidze pansi pano. Yesu akulonjeza kuti:

"Ngati mudzipempha kanthu m'dzina langa, ndidzacita." - Yohane 14:14.

Komabe mapemphero ena amaoneka ngati sakuyankhidwa. Nanga ndi chifukwa chiyani? Pano pali malamulo otsoglera asanu ndi anayi omwe amathandiza kuti mapemphero anu akhale a mphamvu.

(1) Khalani chifupi ndi Khristu nthawi zonse.

"Ngati mukhala mwa Ine, ndi mawu anga akhala mwa inu, pemphani cimene ciri conse mucifuna ndipo cidzacitika kwa inu." - Yohane 15:7.

Pamene tiri pa ubale ndi Mulungu kukhala chinthu choyambirira ndi kukhala ndi lye nthawi zonse, tidzakhala omvetsera ndi oyang'ana kwa lye pa mayankho a mapemphero athu; kupanda apo, titha kukhala osazindikiridwa.

(2) Khalani okhulupirira mwa Mulungu nthawi zonse.

"Ndipo zinthu ziri zonse mukazifunsa m'kupemphera ndi kuhulupirira, mudzalandira." - Mateyu 21:22.

Kukhulupirira, kapena kukhala ndi chikhulupiriro, zitanthauza kuti ife tikuyang'ana kwa Atate wathu wakumwamba yekha kutipatsa zosowa zathu. Ngati mukuvutika ndi kusowa chikhulupiriro, kumbukirani kuti Mpulumutsi wathu anachita zozizwa kwa mwamuna yemwe adalilira kwa lye atasowa

"Pomwepo atate wakumwamba amapfuula, nanena, ndikhulupirira; thandizani kusakhulupirira kwanga." - Mariko 9:24.

Inu yesetsani kuchita ndi chikhulupiriro chimene muli nacho; musadandaule ndi chikhulupiriro chomwe inu mulibe.

(3) Mudzipereke kwathunthu ku cifuniro cha Mulungu.

"Ndipo uku ndi kulimbika mtima kumene tiri nako kwa lye, kuti ngati tipempha kanthu monga mwa cifuniro cace, atimvera." - 1 Yohane 5:14.

Kumbukirani kuti Mulungu akufuna kutiphunzitsa ife, ndiponso kutipatsa ife zinthu, kupyolera mu pemphero. Choncho, nthawi zina lye amayankha kuti, "AYI," nthawi zina amatiolozera kunjira ina yosiyanu ndi kufuna kwathu. Pemphero ndi njira yokhayo yopezera zambiri polumikizana ndi Mulungu ndi chifuniro chake. Tiyenera kusamalitsa kumayankho a Mulungu ndi kuphunzirirapo. Kukhala oyang'anirapo zofuna zathu zenizeni ndi zomwe zimatsatira pa izo zidzakhala zotithandiza.



Mzimu woyeru adzakuthandizani kukhala pa mzere weniweni. "Mzimu amatinenerera oyera ake motsata chifukwa cha Mulungu" (Aroma 8:27). Kumbukirani kuti kufuna kwathu kumatsutsana nthawi zambiri ndi kufuna kwa Mulungu, tikadakhala kuti timaona m'mene lye, Mulungu amaonera.

(4) Dikirani modekha mtima.

"Kuyembekeza ndayembekeza Yehova; ndipo anandilola, namva kupfuula kwanga." - Masalmo 40:1.

Mfundo yeniyeni apa ndi yotilozera ife kuti tiyang'anitsitse pamulungu, ndi mayankho ake. Ndipo

tisamupemphe lye kuti atithandize mphindi imodzi yokha ndi kumuleka kwinako kuti tichite zofuna zathu m'moyo. Dikirani modekha pa Ambuye, tikufunika ife kukhala ndi khaldwe lotere.

(5) Osamatira pa tchimo lina liri lonse.

"Ndikadasekera zopanda pace m'mtima mwanga, Ambuye sakadamvera." - Masalmo 66:18.

Tchimo lodziwika limadula mphamu ya Mulungu m'moyo mwathu; limatilekanitsa ife ndi Mulungu wathu (Yesaya 59:1-2). Simungakangamire pa tchimo ndi dzanja limodzi ndi kufuna mphamu ya Mulungu kuti ithandize ndi dzanja linalo kulapa moona mtima ndi kusiya zochimwazo kumathetsa mavuto athu. Ngati sitiri olola kumpanga Mulungu kuti atimasule ife ku zoipa ndi maganizo oipa, mau oipa, zochita zoipa; mapemphero athu sadzagwira ntchito.

"Mupempha, ndipo simulandira, popeza mupempha koipa, kuti mukazimwaze pocita zikhumbitso zanu." - Yohane 4:3.

Mulungu sadzayankha kuti "INDE) Kwa pemphero lodzikonda

Tcherani khutu lanu lotsegukira kwa Mulungu ndi lamulo lake, chifuniro chake, ndipo lyenso adzatsegula khutu lace kumvetsera madandaulo anu.

"Wopewetsa khutu lace kuti asamve cilamulo ngakhale pemphero lace linyansa." - Miyambo 28:9.

(6) Imvani zomwe Mulungu akuzifuna.

Mulungu amayankha kwa anthu omwe apempha, momuitana lye kuti akhale m'moyo mwawo ndi mphamu yake.

"Odala ali akumva njala ndi ludzu lacilungamo, cifukwa adzakhuta." - Mateyu 5:6.

(7) Musatope ndi kupemphera (pempherani mosalekeza).

Yesu adalongosola za kufunika kwa kupemphera kosalekeza, potiuza nthano ya mayi wamasiye yemwe sadatope ndikupitabe ndi dandaulo lake kwa woweruza. Pa mapeto pake woweruzayu ananena chifukwa chotopersedwa. "Popeza mayi wamasiyeyu akundivutitsa, ndiyesetsa kuti ndipereke chiweruzo choyenera chachilungamo." Ndipo Yesu adamaliza ndi kuti: "kodi Mulungu sadzachita mwa chilungamo kwa osankhidwa ake, omwe alilira kwa lye tsiku ndi tsiku, masana ndi usiku? Kodi adzakhala akuwakhumudwitsa? (Luka 18:5-7).

Kambiranani ndi Mulungu zofuna, ziyang'aniro ndi maloto anu pemphani madalitso apadera, chithandizo munthawi yakusowa. Mufuneni, mumvereni nthawi zonse mpaka mutaphunzira china chake ku mayankho ake a Mulungu.

6. ANGELO AMATUMIKIRA KUZOSOWA ZA IWO AKUPEMPHERA

Wolemba Masalmo adasangalala kuti kupyolera mu utumiki wa angelo a Ambuye, mapemphero ake adayankhidwa.

"Ndinafuna Yehova ndipo anavomera, nandilanditsa m'mantha anga onse... Mngelo wa Yehova azinga kuwacnjiriza iwo akuopa lye, nawalanditsa iwo." - Masalmo 34:4-7.

Pamene tipemphera, Mulungu amatumiza angelo ake kudzayankha mapempherowo (Ahebri 1:4). Mkristu aliyense ali ndi mngelo wake womutsogolera:

"Yang'anirani kuti musanyoze mmodzi wa ang'ono awa; pakuti ndinena kwa inu, kuti angelo ao apenyere cipenyere nkhopo ya Atate wanga wa kumwamba." - Mateyu 18:10.

Chifukwa cha mapemphero athu:

"Ambuye ali pafupi. Musadere nkhwawa konse; komatu m'zonse ndi pemphero, ndi pembedzero, pamodzi ndi ciyamiko zopempha zanu



zidziwika kwa Mulungu. Ndipo mtendere wa Mulungu wakupambana cidziwitso conse, udzasunga mitima yanu ndi maganizo anu mwa khristu Yesu." - Afilipi 4:5-7.

7. UMOYO WA KHRISTU

Bukhu lopatulika limalongsola moyo weniweni wa Mkhristu, monga akunena pa Aefeso 4:22-24, wokhulupirira ayenera "kusiya" moyo wake wakale womwe udadza cifukwa ca "zokhumba zachinyengo," ndi "kuvala" moyo watsopano umene "ulengedwa kufanana ndi Mulungu." Mu malembo awa ndi mu phunziro lathu lotsogolera lija lachisanu ndi chimodzi, tidapeza kuti pakubadwanso mwatsopano ife "timalengedwanso mwatsopano" kukhala munthu wosinthika mwa khristu.

Phunziro ili ndi maphunziro asanu ndi limodzi otsatirawa, akuonetsa moyo wachikristu. Ndipo akutionetsera chinsinsi cha moyo wa chikhristu wokondwa. Zikuthandizaniso inu kumanga ubale wamphamvu ndi khristu, mmene udzathera mu moyo weniweni wapadera wa chikhristu. Chotero yang'anitsitsani pa Yesu lero ndipo mudzatha kukhala mbali imodzi ya chigonjetso chomaliza chachikondwerero pamene mtendere wa khristu udzalamulira popanda woutsutsa.

CHINSINSI CHA CHIMWEMWE

M'chaka cha 1943, mabungwe oona zantchito ku Japan adalamula mazanamazana a anthu a ku Amerika ndi Ulaya kuti akhale "adani," nawasunga m,ndende zina ku China. Adapitirira miyezi yambiri yokhala okha, kukhumudwa, ndi kuhala mopanikizana ndi mantha. Makhalidwe osiyanasiyana apa adakhala limodzi motsutsana, mitima yopsetsana idali pafupipafupi. Timikangano pa zinthu zazin'gono tinakula.

Koma mwamuna m'modzi yemwe andendewa adamutcha "wosakaika, wokondedwa ndi wopatsidwa ulemu ndi wosoweka" - adali Erick Liddell, wachimishoni wochokera ku Scotland.

Mayi wina wadama wa ku Russia m'ndendemo, nthawi ina adakumbukira kuti Liddel anali mwamuna yekhayo yemwe adachita chirichonse kwa iye popanda Malipro. Pamene maiyu adafika m'ndendeyo, yekhayekha atabaidwa, adamuikira iye malo.

Winanso wandende adakumbukira, "iye adali ndi njira yofatsa, ndiyosangalatsira motsitsa mitima ya omwe adali okwiya."



Pamsonkhano wina wa mkwiyo wa andendewa, aliyense ankafuna kuti aliyense wa iwo kapena wina wake wa iwo achitepo kanthu pouza achinyamata an'gono ang'ono omwe amakhala osakhazikika nalowa mmavuto. Liddel adadza ndi yankho. Adakonza masewero, ntchito zamanja, ndi makalasi a maphunziro a ana, nayamba kuhala nawo mwapadera madzulo aliwonse.

Liddel adatchuka nalemenkezedwa pa masewero a Olympic a m'chaka cha 1924, komwe adalandira mendulo ya golidi pa mpikisano wothamanga wa mtunda wa mamitala 400. Koma mumpanipani umenewo, adaonetsa kuhala wopambana mu ulendo wake wa uzimu, nasiriridwa ndi andende ambiri a dziko lapansi.

Kodi chidamupangitsa iye kuhala wapadera chonchi ndi chiyani? Mutha kupeza zinsinsi zake pa ola lachisanu ndi chimodzi m'mawa uliwonse. Iyi idali nthawi yomwe amadzuka ndikuyenda moyang'anu kudutsa andende anzake akugona, napita pa gome, nayatsa muuni waung'ono kuti aone m'kabukhu kake kakang'ono ndi Bukhu lopatulika. Eric Liddel adapeza chisomo ndi mphamvu tsiku ndi tsiku mu chuma cha mawu a Mulungu.

1. BUKHU LOTSOGOLERA MOYO WA CHIKRISTU




Bukhu lopatulika lidalembedwa ngati lotsogolera kwa m'khristu liri lodzala ndi nthano zenizeni za anthu monga ife tomwe omwe adakumana ndi zobetchera ngatinso zomwe tikukumana nazo ife tsiku ndi tsiku. Podziwa anthu amenewa zisoni zayo ndi zisangalalo zayo, mavuto awo ndi mwayi wao-zitithandiza kukula ngati akhristu.

Davide, wolemba Masalimo akuonetsera chithunzithunzi cha mmene moyo wathu watsiku ndi tsiku uyenera kukhalira wodalira pa Mawu a Mulungu pouyerekeza moyowo ndi kuwala kwa muuni:

"Mau anu ndiwo nyali ya kumapazi anga, ndi kuunika kwa panjira panga." - Masalimo 119:105.

Kwala komwe timakupeza tsiku liri lonse kuchokera mu Baibulo kumapangitsa kuonetsera poyeria makhalidwe omwe tiyenera kukhala nawo m'moyo mwathu ndi zofunikira kuti tikule muuzimu. Mwa zonse, Baibulo limationetsera ife ngati Yesu akuwalira pa moyowo.

2. UBWENZI WAKUSINTHA



Khristu akufuna kuti Bukhu lopatulika kuti likhale lenileni kwa inu monga kalata yolembera inu kuchokera kwa bwenzi lapamtima.

"Sinditchanso inu akapolo; cifukwa kapolo sadziwa cimene mbuye wace acita; koma ndacha inu abwenzi; cifukwa zonse zimene ndazimva kwa Atate wanga ndakudziwitsani." - Yohane 15:15.

Yesu amatifunira ife zabwino zokhazokha komanso amayembekeza zabwino zokhazokha komanso amayembekeza zabwino koposa mwa ife. Mawu ake amatibweretsa ife mundandanda wa Mulungu: anthu amene lye awadalira ndikuwadzudzula paokha.

"Zinthu izi ndalankhula ndi inu, kuti mwa Ine mukakhale nao mtendere. M'chibvuto, koma limbikani mtima." - Yohane 5:33.

Ngati mufuna kukhala nawo mtendere umenewu ndiubale wotetezedwa umenewu ndi Khristu, tiyenera kuwerenga mukalata yomwe atitumizira ife. Umu ndi momwe Baibulo liliri kukambirana kochokera kumwamba. Musalole kuti makalata amenewa akhale osatsegulidwa. Uthenga wakusintha umene uli m'menemo ndi umene uli wofunika kwa ife.

Apa pali umboni wodziwika bwino wa mphamu ya Baibulo. "Ndidafuna thandizo ndipo ndidalipeza mwa Yesu. Chirichonse chofunika andipatsa, njala ya m'moyo mwanga anaithetsa; Baibulo kwa ine liri chivumbulutso cha Khristu. Ndikhulupirira Yesu chifukwa ndi Mpulumutsi woyera. Ndikhulupirira Baibulo chifukwa ndapeza kuti iloli ndi liu lochokera kwa Mulungu kudza ku moyo wanga." - Utumiki wa kuchiza, tsamba 461.

3. ZOTSOGORERA KUKHALA MOYO WA MAWU A BAIBULO NDI MALAMULO KHUMI

Poonetsetsa Malamulo khumi a Mulungu kumathandiza kumvetsa chifukwa chomwe malamulowo ndi Baibulo ziri zofunika ndi zosatha pa kakhalidwe kathu.

Malamulowa amagawidwa pawiri. Gavo loyamba limanthauzira ubale wathu ndi Mulungu. Ndipo liri ndi malamulo anayi Gavo lachiwiri la Malamulo asanu ndi limodzi litanthauzira ubale pakati pa munthu ndi m'zake. Onsewa akupezeka pa Eksodo 20:3-17.

Malamulo awiri oyambirira akuonetsera ubale wathu ndi Mulungu ndi kumulambia.

- (i) Usakhale nayo Milungu ina koma Ine ndekha"
- (ii) "Usadzipangire iwe wekha fano losema...usazipembedzere izo, usazitumikire izo...."
- Lamulo lachitatu ndi lachinayi likuonetsera ubale wathu pa dzina la Mulungu ndi tsiku lake loyera.
- (iii) Usachule dzina la Yehova Mulungu wako pacabe;
- (iv) Uzikumbukira tsiku lasabata likhale lopatulika. Masiku asanu ndi limodzi uzigwira ndi kumariza ntchito zako zonse, koma lachisanu ndi chiwiri ndilo Sabata la Yehova Mulungu wako"
- Lamulo lachisanu ndi chiwiri limatchinjiriza ubale wa mabanja.
- (v) "Uzilemekeza atate wako ndi amako; kuti acuru ke masiku ako m'dziko amene Yehova Mulungu wako



akupatsa iwe."

(vi) Usacite cigololo."

Lamulo lachisanu ndi chimodzi, lachisanu ndi chitatu, lachisanu ndi chinayi ndi lakhumi amatiteteza ife mu chikhalidwe chathu ndi anzathu.

(vii) "Usaphe."

(viii) "Usabe."

(ix) "Usamnamizire m'nzako."

(x) "Usasirire nyumba yace ya mnzako, usasirire mkazi wace wa mnzako... kapena kanthu kali konse ka mnzako."

Malamulo khumi amaonetsera ubale wathu kwa Mulungu komanso kwa anthu ena. Iwo ali otitsogolera mu moyo wauzimu.

4. ZOMWE YESU ADANENA PA ZA MALAMULO KHUMI

Tsiku lina Yesu akuphunzitsa, mnyamata wachidwi kwambiri adamthamangira iye namufunsa, "mphunzitsi, kodi ndingachite chiyani chabwino kuti ndipeze moyo wosatha?" (Mateyu 19:16). Khristu anatha kuona kuti mnyamatayu chuma chakecho "ndikumvera malamulo kuwatsata" (vesi 17).



Mnyamata anayesetsa kuti Yesu asaone bvuto lapandalama lomwe adali nalo, napitiliza kufunsa za lamulo lomwe liri loposa onse, kuti iye alitsate. Yesu adamuyalira angapo mwa Malamulo khumi (vesi 18,19).

Pamapeto pake, mnyamata "mwini chumayu" adakhumudwa nachokapo (mavesi 20-22). Amatha kuwadziwa malamulowo koma samatha kudziwa mzimu womwe udali m'malamulowo kuti akafike posiya kudzikonda kwake m'moyo.

Malamulo khumi amationetsera ife malire omwe afikiridwa ndi ubale weniweni ndi Mulungu komanso anthu. Yesu anaonetsera kuti kumvera kuti kuli njira yakuchisangalalo chenicheni.

"Ngati musunga Malamulo anga, mudzakhala m'chikondi canga; monga lne ndasunga Malamulo atate wanga, ndipo ndikhala m'chikondi cace. Izi ndalankhula ndi inu, kuti chimwemwe canga cikhale mwa inu, ndikuti chimwemwe canu cidzale." - Yohane 15:10, 11.

5. CHOTSOGOLERA KU MOYO WOKONDWA

Bukhu la Mlaliki ndi dongosolo loperekedwa lazofufuza zomwe Solomoni adafufuza zokhuza kukondwa. Iye adalemba zakukondwa mu chuma cha dziko lapansi: nyumba zokongola, minda yakupatsa zakucha zambiri, minda yokongola, ndi m'minda yazipatso zobala zokoma. Anaonjezera antchito. Napeza kuti iye ali nazozonse zofunika pa moyo wamunthu. Komabe adapezeka wosakondwa, ndipo analembala kuti:

"Pamenepo ndinayang'ana zonse manja anga anazipanga, ndi ntchito zonse ndinasankha pozigwira, ndipo taona, zonse zinali zacabecabe ndi kungosautsa mtima, ndipo kunalibe phindu kunja kuno." - Mlaliki 2:11.

Solomoni tsono adafufuzabe ndicholinga chopeza chisangalalo m'dziko lapansi. Analedzera, nakhala ndi akazi, naimba nyimbo. Pamapeto pake analembala:

"Cabe zacabetu, ati Mlalikiyo; zonse ndi cabe." - Mlaliki 12:8.

Solomoni adapeza kuti Ambuye ndi wabwino. Poyerekeza moyo wake woyamba wakumvera Mulungu ndi moyo wake wina wakufuna kukondwa mu zinthu za uchimo, adalembano:

"Mau atha; zonse zamveka zatha; opa Mulungu, musunge malamulo ace; pakuti coyenera anthu onse ndi ici." - Mlaliki 12:13.

Solomoni adaona ngati andapeze chifupi chake cha moyo wokondwa mkatì mwa nyama zakutchire. Kumapeto kwa moyo wake, iye adali munthu wotha kuvomera kulakwa kwake ndipo adalemba kuti: **"koma wosunga cilamulo adalitsika." - Miyambo 29:18**

6. MALAMULO KHUMI NDI CHIPANGANO CHATSOPANO CHOSATHA

M'chipangano chatsopano, Yakobo akuchitira umboni kuti:

"Pakuti amene aliyense angasunge malamulo onse, koma akakhumudwa pa limodzi, iyeyu wacimwira onse. Pakuti iye wakuti, "usacite cigololo, anatinso, "usaphe" ndipo ukapanda kucita cigololo, koma ukapha, wakhala wolakwira lamulo. Lankhulanî motero, ndipo citani motero, monga anthu amene adzaweruzidwa ndi lamulola ufulu." - Yakobo 2:10-12.

Wolalikira wina wotchuka wakale wotchuka wachi Baptist, dzina lace Charles Spurgeon, adalalika, "lamulo la Mulungu ndi loyera, lakumwamba, ndi langwiro...palibe lamulo lalikuru, kapena laling'ono, koma ndilosayerekezeka mu Umulungu wake ndi umboni wake."

John Wesley, m'modzi wa omwe adayambitsa mpingo wa Methodist, adalemba izi zokhudzana ndi chipiliro cha chilamulo: "m'chilamulo cha chikhaldwe munali malamulo khumi...lye (khristu) sanachititsepo...mbali iri yonse ya lamulo liyenera kukhala chikhaliire kwa anthu onse kumibadwo yonse."



Billy Graham, wolalikira wotchuka kwambiri padziko lapansi, amawatenga Malamulo khumi kukhala akuya ndipo adalemba bukhu lonse lokhudzana ndi kufunika kwake ku moyo wa chikhristu.

7. MPHAMVU YA KUMVERA

Bukhu lopatulika ndi malamulo khumi sizisinha, ndipo siziderekezedwa, ndiponso ziri zotsogolera mwangwiro ku moyo wachisangalalo. Komabe mitima iri yosakhazikika ndipo iri pachimkangano.

Mayi wina adalongosola motere: "ndikhulupirira kuti malamulo khumi amamanga, ndiri ndi umboni kuti kusunga malamulowa kumabweretsa chisangalalo. Ndayesera ine ndi moyo wanga wonse kuwasunga koma ndikulephera. Ndayamba kukhulupirira kuti palibenso angathe.



Khalidwe la munthu liri loti ayesere kusunga malamulo a Mulungu. Koma yankho la kuyesera konseko ndi kukhumudwa nthawi zonse mumtima wa munthu, "sindingathe kumvera!" Chifukwa chiyani?

"Cifukwa cisamaliro ca thupi cidana ndi Mulungu; kutero." - Aroma 8:7.

Kodi cholinga cha malamulo khumi a Mulungu ndi chiyani?

"Pakuti ucimo udziwika ndi lamulo." - Aroma 3:20.

Ntchito yalamulo ndi kutitsogolera kukuzindikira kuti tiribe chiyembekezo chifukwa tidataika muuchimo, ndipo tisowa mpulumutsi.

"Momwemo cilamulo cidakhala namkungwi wathu wakutifikitsa kwa Khristu, kuti tikayesedwe olungama ndi cikhulupiro." - Agalatiya 3:24.

Yesu ndi yankho! Nthawi ina yakebe timapezeka tiri osowa chiyembekezo pampapazi a Yesu, ndipo mwa chikhulupiro titha kulandira chikhulukiro cha machimo athu ndi mpahmvu yakwa lye kuti ticasunge ndi kumvera malamulo ake.

8. KUMVERA KWA CHIKONDI KU MALAMULO KHUMI

Yesu akutiua ife kuti kumvera ndi zotsatira za chikondi:

"Ngati mukonda Ine sungani malamulo anga." - Yohane 14:15.

Ngati tikonda Mulungu, tidzamumvera ndi kusunga malamulo anayi oyambirira omwe akunena za ubale wathu ndi Mulungu; ndipo ngati tikonda anthu anzathu, tidzasunga Malamulo asanu ndi limodzi omalizirawo omwe amonetsera ubale wathu ndi ena.

Munthu yemwe akhumudwa pa malamulo khumiwa achimwa:

"Yense wakucita cimo acitanso kusayeruzika: ndipo cimo ndilo kusayeruzika." - 1 Yohane 3:4.

Koma tithokoze Mulungu, tiri ndi Mpulumutsi yemwe adadza kudziko lapansi natifera, naukitsidwa, ndipo ali ndi moyo ndi cholinga chimodzi.

"Ndipo mudziwa kuti Iyeyu anavomera kudzacotsa macimo, ndipo mwa lye mulibe cimo." - vesi 5.



Mpulumutsi wathu amakhululukira ndi kucotsa kucimwa kwathu (1 Yohane 1:9). Ndipo akulonjeza kutipatsa ife moyo wachilikati weniweni: wodana ndi kudzikonda nditchimo:

"Cifukwa cikondi ca Mulungu cinatsanolidwa m'mitima mwathu mwa Mzimu woyera, amene wapatsidwa kwa ife." - Aroma 5:5.

Tiribe ife chotiyenereza kuti tingasunge malamulo a Mulungu chikondi cha Mulungu "chotsanolidwira...m'mitima yathu" ndicho chiyembekezo chathu chokha.

9. CHISOMO CHA MULUNGU NDI KUMVERA KU CHILAMULO

Chipulumutso ndi mphatso. Sitingathe kuchigwirira ntchito. Ife tingathe kungochilandira kwa ulere mwachikhulupiro. Timalungamitsidwa (kukhala woyenera pamaso pa Mulungu) ngati mphatso kupoyolera mu chikhulupiro chokha basi chifukwa cha chisomo cha Mulungu.

"Pakuti muli opulumutsidwa ndi cisomo cakucita mwa cikhulupiro, ndipo ici cosacokera kwa inu: ciri mphatso ya Mulungu." - Aefeso 2:8.

Sitingathe kusunga malamulo mwantchito zathu poyesetsa sitingathenso kusunga malamulo kuti tikapulumuke. Koma tikadza kwa Yesu mwa chikhulupiro ndi kudzipereka ndi kupulumutsidwa, chikondi chake chimadzala mu mitima yathu. Zotsatira za mphamvu ya umulungu iyi ya cisomo ndi kulandira, tifunika kumtsatira lye ndi kumumvera lye kupyolera mu mphamvu ya chikondi chake m'mitima yathu (Aroma 5:5).

Paulo akutsimikizira kulephera kwa umunthu mukuyesetsa kwake ndikutionetsera kuti pansi palamulo ngati njira ya chipulumutso, koma "pansi pa cisomo" ndipo

"Tidzacimwa kodi cifukwa sitiri alamulo, koma a cisomo? Msatero ayi" - Aroma 6:15.

Chifukwa chiyani? Pakuti mtima wodzazidwa ndi chikondi umabala moyo wacikondi chakumvera! (Aroma 13:10). Kukonda Khristu ndiye kumvera lye.

"Iye wakukhala nao malamulo anga, ndi kuwasunga, iyeyu ndiye wondikonda Ine." - Yohane 14:21.

Eric Liddel akuonetsera kuti, ngakhale munthawi yovuta, wokhulupirira amene wazikika mwa mphamvu ya Mulungu amakhala wokwanitsidwa, ndi womvera. Liddel akutionetseranso chisomo chakugonjetsa nthawi ya chisautso ndi mantha. Ubale wake wachikondi ndi Yesu Khristu udampatsa mphamvu za mzimu woyerwa, ndi kumupangitsa iye kukumana ndi "zofunika zachilungamo za chilamulo" (Aroma 8:1-4).

Ubwenzi wachikondi ndi Mpulumutsi wopachikidwa woukitsidwa umabweretsa moyo wamtengo wapatali. Kodi inu mwapeza chinsinsi ichi mwa inu nokha? Chikondi cha Yesu pa inu chidampangitsa lye kupereka moyo wake chifukwa cha machimo anu. Akudzipereka kukupatsani mphamvu mu ubale wanu ndi chikondi chake ndi ku "kukhwimitsani ndi zonse zabwino kuti mukachite chifuniro chake" (Ahebri 13:21). Kodi mukuyankha bwanji?



CHINSINSI CHA MPUMULO WA KUMWAMBA

Zaka za m'mbuvo zapitazo ena anali kunenera za mtsogolo kuti posachedwa tikhala nayo nthawi ya mtambasale yambiri yomwe sitikhoza kuigwiritsa ntchito moyenera. Panali zifukwa zabwino zonenera motsimikiza motere. M'mizinda ya pa dziko lapansi lero makina a komputa akugwira ntchito yomwe ikanagwiridwa mwezi wathunthu mu mphindi zowerengeka zokha basi. Zifanizo zokhala ngati anthu zayamba kugwira ntchito zolemetsa m'malo ogwirira ntchito.

Koma ma komputa atatha kuonetsa changu chawo ndi makina ongoyenda okha anthu akhala odabwa kwambiri kusiyana ndi kale anthu nthawi yakhala ili kuwacheperabe. Pamwamba pa zonse nawo mabanja nthawi ili kuwacheperabe. Abambo ndi Amayi akuona kuti nkolimba kuti apeze "Nthawi yopambana" ndi ana koma imapezeka yosakwana.

Kafukufuku adachitika m'dera lina adapeza kuti nthawi yomwe Bambo pabanja lake amakhala pamodzi ndi ana ake patsiku ndoyokwana mphindi ya masekondi makumi atatu mphambu zisanu ndi ziwiri (37 seconds) nawo mabanja akukhalanso opanda nthawi yokhalira pamodzi ndikukhudzana.

Nanga tingachitenji kuti tiyambe kukhalira pamodzi ndi kumakhudzana?

1. MANKHWALA OCHOTSERA MOYO WOTANGANIDWA

Yesu amamvetsetsa mavuto omwe amakhala ndi mabanja omwe amatanganidwa kwambiri namasowa nthawi ndipo lye (Yesuyo) akufuna kuti timvetsetse mpumulo wauzimu omwe uli mbali ya moyo wopambana.

"Idzani kuno kwa Ine nonsenu akulema ndi akutodwa ndipo Ine ndidzakupumulitsani inu.....phunzirani kwa Ine chifukwa ndiriwofatsa ndiwodzicepetsa mtima ndipo mudzapeza mpumulo wa miyoyo yanu." Mateyu 11:25,29.

Baibulo likutifotokozena kuti mpumulo wa Uzimu uwu umapezeka njira ziwiri. Kubwera kwa Khristu tsiku liri lonse kapena kubwera kwa Khristu mlungu uli wonse.

2. KULUMIKIZANA NDI YESU TSIKU LIRI LONSE

Makamu a anthu anadza kawiri kawiri ali kufuula kufuna kuti Yesu awachitire kanthu koma Khristu ananena nawo mwa mtendere ndi mwa mzimu wofatsa kwa aliyense womuzungulira lye. Njira yotani? Analu kukhala ndi nthawi ya padera yolankhulana ndi Atate ake tsiku liri lonse. lye anadalira pa Atate ake kosalekeza kuti apeze njira zopezera zobetchera za m'miyoyo ya anthu. (Yohane 6:57).

Ngati ife tifuna kukhala ndi moyo wopambana wokhala ngati umene lye anakhalira tiyenera ife nthawi zonse kudalira pa Yesu - tilole Mawu Ake ndi Mzimu wake atidzaze ndi kutiumba ife. Njira yoposa yofuna kutithandiza ife pokomana nayo mivi yoyaka moto ya mdierekezi aliyense payekha ndi kutilekanitsa ndi mabanja athu ndiyo yopeza nthawi yabwino yomakomana naye Khristu, amatiuza kuti:



"KHALANI MWA INE, ndi Ine mwa inu Pakuti kopanda Ine simungathe kucita kanthu. (Yohane 15:4,5) Chosowa chachikulu munthawi yathu ino,ndi njira zopezera zinthu za Uzimu zomwe zimapezeka kupyolera mu chiyanjano chathu ndi Khristu tsiku ndi tsiku".

Nsonga yopambana yomwe ifunika kutsimikizidwa yonena za chiyanjano chathu ndi Khristu ndiyo ntchito yake yomwe anaimaliza pa mtanda, kupumula koona, chitetezo chenicheni, chiyenera kukhala chifukwa cha kutsiriza kwakukulu kumene Yesu anakunena pamene lye anaafuula, pamene lye anali kufa. "KWATHA" (Yohane 19:30) M'mawu ena. Ntchito Yake ya chiombolo idatsirizika.



"Koma tsopano (Khristu) KAMODZI PA CHITSIRIZO CHA NTHAWIZO waonekera... KUCHOTSA UCHIMO mwa nsembe ya lye yekha". Ahebri 9:26.

Pamene Yesu anafa, "anachotsa uchimo". Ndiye chifukwa chake adanena kuti wokhulupirira amene avomereza machimo ake akhoza "kupumula" mu ntchito yomalizidwa ya Khristu. Ife tidalandiridwa.

Uchimo umapezeka titatha kusangalala kapena kumva kupweteka m'miyoyo yathu lero. Koma Yesu anathana nawo uchimo, kamodzi kwa nthawi zonse pamtanda. Kulira kwa Yesu "Kwatha", kunatsekera lonjezo lake lakuti "Ine ndidzakupumulitsani inu" ndi mawu oona. Khristu adamaliza ntchito ya chiombolo cathu pa Karivale. (Tito 2:14) kotero kuti anapumula m'manda pa Sabata nauka kuchokera m'mandamo pa tsiku loyamba la pa mlungu (Sunday) m'mawa monga WOGONJETSA uchimo ndi imfa.

Palibe china chopambana koposa kwa M'Khristu ngati mpumulo mu ntchito yake yomalizidwa ya Khristu.

"Tiyandikire ndi mtima woona M'CHIKHULUPIIRO CHOKWANIRAtigwiritse chibvomerezo chosagwedera cha chiyembekezo chathu pakuti WOLONJEZAYO ALI WOKHULUPIRIKA." Aheberi 10:22,23.

Chifukwa "Wolonjezayo ali wokhulupirika" tingathe kulowa mu mpumulo wa chipulumutso umene Yesu adalonjeza. Kukhazikitsidwa, mtendere, ndi mpumulo umene timaupeza mwa Yesu tsiku liri lonse sichifukwa cha kena kali konse komwe tichita, koma ndi chifukwa cha zomwe lye anachita pa mtanda.

Tingathe kupumula mwa Khristu chifukwa anatitsimikizira chipulumutso chathu, chitsimikizo chimenechi chimatidzutsa ife kukhala ndi Khristu tsiku liri lonse, kudya mawu Ake ndikumapuma mpweya wochokera kumwamba kupyolera mu pemphero. Kukomana kwathu ndi Yesu m'malo opemphera kumatithandiza ife kubwezedwa ku moyo wotanganidwa ndi zinthu zadziko kupita ku moyo wamtendere ndi woyeria.

3. KULUMIKIZANA NDI KHRISTU MLUNGU ULI WONSE



Khristu atatha kulenga dzikoli masiku asanu ndi limodzi (Akolose 1:16,17) Anapereka tsiku la Sabata kukhala lopumula. Ndi nthawi yoikika pa mlungu uli wonse kuti ife tidzilumikizana naye Khristuyo.

"Ndipo anaziona Mulungu zonse zimene anazipanga ndipo, taonani, zinali zabwino ndithu. Ndipo panali madzulo ndipo panali m'mawa, tsiku lachisanu ndi chimodzi. Ndipo zinatha kupangidwa zakumwamba ndi dziko lapansi, ndi khamu lao lonse. Tsiku la chisanu ndi chiwiri Mulungu anamaliza ntchito yonse anaipanga;

ndipo ANAPUMA tsiku lachisanu ndi chiwiri, ku ntchito yake yonse Mulungu ndipo ANADALITSA tsiku lachisanu ndi chiwiri, NALIYERETSA LIMENELO chifukwa limenelo adapuma ku ntchito yake yonse imene Mulungu anailenga ndi kupanga" - Genesis 1:31-2:1-3.

Monga Mlengi wao, Yesu "anapumula" mu Sabata yoyamba ndi Adamu ndi Hava ndipo lye "analadalitsa" tsiku la Sabatalo ndi "Kuliyeretsa". Mulungu anapanga masiku asanu ndi awiri pa mlungu kuti adzizungulira, osati chifukwa cha phindu lake, koma chifukwa cha Adamu ndi Hava ndi kwa ifenso lero. Chifukwa lye anawasamalira anthu awo anawalenga, lye analinganiza kuti tsiku liri lonse la chisanu ndi chiwiri kupyolera mu miyoyo yawo yonse lidziperekedwa kumufuna Mulungu. Sabata liri lonse liyenera kumakhala lopumula kuti thupi ndi kuuzimu komwe. Kulowa kwa uchimo m'dziko lathu lino kwapangitsa kupumula pa tsiku la Sabatali kuhkala kovuta.

Mpulumutsi yemwe uja adalonjeza Adamu ndi Hava "mpumulo," patatha zaka zikwi ziwiri mtsogolo mwake anaperekanso lamulo kwa Mose pa phiri la Sinai (1 Akorinto 10:1-4) Yesu anasankha mpumulo wa Sabata pakati pa Malamulo, pakati peni peni pa mtima wa Malamulo Khumi. Lamulo la chinayi limati:-

"UZIKUMBUKIRA TSIKU LA SABATA LIKHALE LOPATULIKA. Masiku asanu ndi limodzi uzigwira ndi kumaliza ntchito zako zonse, koma tsiku la chisanu ndi chiwiri ndilo Sabata la YEHOVA Mulungu wako; usagwire ntchito iri yonse, kapena iwe wekha, kapena mwana wako wa mwamuna, kapena mwana wako wamkazi, kapena wantchito wako wamwamuna, kapena wa ntchito wako wamkazi, kapena nyama zako, kapena mlendo amene ali m'mudzi mwako, chifukwa masiku asanu ndi limodzi Yehova adamaliza zakumwamba ndi zapansi, ndi nyanja, ndi zinthu zonse ziri m'menemo, napumula tsiku la chisanu ndi chiwiri chifukwa chache Yehova anadalitsa tsiku la Sabata kuti likhale lopatulika." Eksodo 20:8-11.

Mulungu anakhazikitsa Sabata monga tsiku "lomalikumbukira" Yehova amene "anapanga kumwamba ndi dziko lapansi" Mpumulo wa Sabata mlungu uli wonse umalumikizana ndi Mlengi yemwe anadalitsa tsiku ili nalipatula.

Pamene Yesu anali pa dziko lino lapansi lye anapeza mwayi womalumikizana ndi Atate wake tsiku liri lonse. Iye anali kupeza mwayi kupyolera mkupumula kwake kwa pa Sabata, pomapita kukapembedza pa dzuwa la Sabata, Luka amatiuza kuti :-

"Ndipo anadza ku Nazarete, kumene analeredwa; ndipo TSIKU LASABATA analowa m'sunagogue, MONGA ANAZOLOWERA" - Luka 4:16.

Ngati munthu wa umulungu Yesu anafuna kumapumula pa tsiku la Sabata pamaso pa Atate Wake. Ife monga anthu a m'thupi la nyama tiyenera kumapumula koposa pamene Yesu anatsutsa miyambo yoikidwa ya a Yuda yonena za Sabata (Mateyu 12:1-12) (Yesu) anawauza kuti Mulungu anaika Sabata kuti anthu adzilumikizana ndi lye.

"Ndipo ananena nao, Sabata linaikidwa chifukwa cha munthu, simunthu chifukwa cha Sabata; motero Mwana wa munthu ali mwini dzuwa la Sabata lomwe." - Marko 2:27, 28.

Yesu anaonetsa kufunika kwake kwa Sabata ngakhale pa imfa yake. Iye anafa tsiku lokonzekera, (Friday) "tsiku lokonzekera Sabata iri pafupi kuyamba." (Luka 23:54) Pa nthawiyo, lye anati, "Kwatha", ndiye kuti ntchito Yake yobwera ku dziko lino lapansi kudzafera mtundu wonse wa anthu ochimwa (Mlowamalo) inatha (inamalizidwa) (Yohane 19:30 4:34; 5:30). Kukondwerera kutsirizika kwa ntchito Yake, Yesu anapumula m'manda pa tsiku lonse la Sabata.

Khristu atangotsiriza ntchito yake yakulenga patsiku lachisanu ndi chimodzi napumula tsiku lachisanu ndi chiwiri, kupyolera mu imfa Yake ya pamtanda anatsiriza ntchito Yake yakutiombola pa tsiku lachisanu ndi chimodzi, napumula tsiku lachisanu ndi chiwiri.

Tsiku loyamba lapa mlungu (Sunday) anauka m'manda, Mpulumutsi wogonjetsa (Luka 24:1-7) lye anawauza akuphunzira ake kusunga Sabata ngakhale ati adzakomane nawo mavuto atauka lye. Polankhula za kuonongedwa kwa Yerusalem kumene kunachitika patangotha zaka makumi anayi (40) lye atauka kwa akufa, anawalamulira kuti :

"Ndipo pempherani kuti kuthawa kwanu kusakhale pa nyengo ya chisanu, kapena pa Sabata." - Mateyu 23:20.



Mpulumutsi wathu adafuna akuphunzira Ake ndi otembenuka kupitiriza kuchita zomwe lye anawaphunzitsa iwo (Yohane 15:15, 16) lye anafuna iwo kuchita nawo mpumulo wa chipulumutso ndi mpumulo wa Sabata. Iwo sanamugwiritse lye mwala. Akuphunzira anapitiriza kusunga Sabata itatha imfa ya Yesu. (onani Luka 23:54-56; Machitidwe 13:14; 16:13; 17:2; 18:1- 4.)

Mtumwi wokodendwa, Yohane anasunga chilumikizano chake cha mlungu ndi mlungu ndi Khristu pa dzuwa la Sabata liri lonse. M'masiku ake am'tsogolo analemba chotere: Ndinagwidwa ndi Mzimu tsiku la Ambuye". (Chibvumbulutso 1:10). Molingana ndi Yesu, "Tsiku la Ambuye" ndilo tsiku la Sabata, "Pakuti Mwana wa munthu ali mwini tsiku la Sabata" Mateyu 12:8).

Pa Sabata timakondwerera zinthu ziwiri zazikulu zomwe anatsiriza Yehova m'malo mwathu: Kutilenga ndi kutipulumutsa ife. Machitachita a Sabata adzapitirira kuchitikabe kumwamba.

"Pakuti monga m'mwamba mwatsopano ndi dziko lapansi latsopano limene ndidzalenga, lidzakhalabe pamaso pa Ine ati YEHOVA kuyambira pa Sabata lina kufikira ku linzace anthu onse adzafika kudzapembedzera pamaso pa Ine, ati YEHOVA." Yesaya 66:22, 23.

4. PHINDU LA MPUMULO WA SABATA

Anthu lero alikuponderezana wina ndi m'nzake m'miyoyo yaho. Anthu ali kutha, mabanja ali kutha kulekana. Koma Mulungu akupereka Sabata ngati njira yabwino koposa pofuna kukhala ndi moyo wabwino.

Tiyeni tione zina zomwe timapeza mu mpumulo wa Sabata:

(i) SABATA NDI CHIKUMBUTSO CHA CHILENGEDWE, PAKULISUNGA ILO KUKHALA LOPATULIKA TIMAKUMBUKIRAMLENGI WATHU. Maora ake opatulika amapereka nthawi yodabwitsa yokhudzana ndi miyoyo yathu dziko limene Mulungu adalilenga. Ndi nthawi iti yomaliza imene inu kapena banja lanu munatenga nthawi yoyenda munkhalango yokongola ya chete kapena kuyenda mbali mwa mtsinje wopita m'matanthwe? Sabata limatipatsa ife nthawi yokaona chilengedwe cha Mulungu ndikuona zodabwitsa zomwe lye anatilengera ife.

(2) PASABATA TIMAPEZA CHIMWEMWE CHA KUPEMBEDZA NDI CHIYANJANO NDI AKHRISTU ANZATHU Pali phindu pakupembedza Mulungu ndi anzathu monga gulu lopembedza Sabata limatipatsa ife nthawi yapadera yokumana pamodzi monga thupi la mpingo kudzutsa mphamvu zathu za Uzimu.

(3) SABATA LIMAPERERA NTHAWI YAKUCHITA NTCHITO ZOKOMA MTIMA KWA ENA. Mwina nzanu woyandikana naye wakhala ali kudwala pakati pa mlungu pamene inu munalibe nthawi yokamuona ndi kumuchezera. Pamene bwenzi limasowa wina



womumvetsera mavuto ake chifukwa cha imfa ya mwamuna wake. Chifukwa chakusowa kwanu nthawi pakati pa mlungu koma mukakamuona la Sabata akakuuzani inu mavuto ake Yesu ati, "Nkololeka kuchita zabwino tsiku la Sabata." (Mateyu 12:12)

(4) **SABATA NDI TSIKU LOLIMBIKITA MABANJA** Pamene Khristu analamulira kuti. "Pa Sabata, usagwire ntchito iri yonse." (Eksodo 20:10) Iye sakadapereka magwiridwe a ntchito oyenera kwa Amuna ndi Amayi osapuma pa ntchito oposa awa, Sabata ndi chim'phona choimitsa mabanja. Sabata ndi tsiku limodzi lokha m'mene tingaike m'malo motanganidwa kuikamo mapemphero, m'malo mogwira ntchito, kumangosangalala ndi kukhala mwachete. Mpumulo wa Sabata umapereka kubanja lonse nthawi yolumikizana ndi Khristu ndikupeza kwa lye mphamvu za Uzimu.

(5) **SABATA NDI NTHAWI PAMENE YESU AMABWERA PAFUPI NANU.** Chiyanjano chiru chonse chimafunika kumakhala ndi nthawi yopambana yapadera, ndipo chiyanjano chathu ndi Khristu chiyeneranso kukhala nayonso nthawi yotero. Kulipereka tsiku lonse kwa Khristu mlungu uli wonse ndi njira yokha yopambana yosungira ubwenzi wathu ndi lye kukhala wokondweretsa.

Sabata limatipatsa ife nthawi yoonjezera, yophunzira mawu a mu Baibulo, ndi nthawi yopemphera, nthawi yoonjezera yokhala wekha ndiKhristu pa malo achete ndi kumvetsera.

Yesu "anadalitsa tsiku lachisanu ndi chiwiri naliyeretsa limenelo." Ndi lonjezo lakupeze ka kwake. (Genesis 2:3) Mukhoza kumvetsetsa chifukwa chake kuli kofunika kumasunga tsiku lachisanu ndi chiwiri (Saturday) lomwe liri Sabata, chifukwa ndi tsiku limene Khristu analipatula panthawi ya chilengedwe kuti alumikizane ndi ife m'njira yapadera.

Pamene Yesu analenga Sabata zimakhala ngati anali ndi maganizo ku mbadwo wathu uno. Ndi zeni-zeni zomwe tisowa mu nthawi yathu yotanganidwa yotere: Tsiku leni - leni lomwe timapuma ku kena kali konse; tsiku lopembedza Mulungu, kukhudzana ndi chilengedwe, ndi kutsimikizira pa chiyanjano m'malo mwa zinthu, SABATA.

5. KULAWA ZA MPUMULO WA KUMWAMBA

Tingathe kuwerengera phindu lonse lolumikizana ndi Yesu kupyolera mkukumana kwathu ndi lye tsiku ndi tsiku mlungu ndi mlungu mu liwu limodzi - mpumulo. Liwu "Sabata" limachokera mu chiheberi kutanthauza mpumulo, sichodabwitsa kuti malembo amatchula tsiku lachisanu ndi chiwiri, "Sabata lakupumula" (Levitiko 23:3)

"Mulungu) pakuti wanena za tsiku la chisanu ndi chiwiri ndipo Mulungu anapumula tsiku la chisanu ndi chiwiri kuleka ntchito zake zonse;MOMWEMO UTSALIRA MPUMULO WA SABATA WA KWA ANTHU A MULUNGUchifukwa chake tichite changu cha kulowa mpumulowo" - Aheberi 4:4-11.

Pakuchita chita nawo mpumulo wa Sabata zimatipatsa ife kulawa mlungu ndi mlungu za chimwemwe chomwe tidzakhale nacho mu mpumulo wa kumwamba kweni-kweni.

Mpumulo umenewu si moyo wa mtambasale ai; zimatanthauza kuchinjirizidwa, mtendere ndi moyo wabwino umene ukapezeke patsinde pa moyo wambiri wosatha. Mtundu uwu wa mpumulo wa Uzimu ukhoza kuyamikiridwa kupyolera m'machita chita. Umboni wa awo amene akomana nawo machita chita a mpumulo wa chipulumutso ndi mpumulo wa Sabata. "Ngati mungalowe mumpumulo wa Yesu kupyolera



mkulumikizana ndi lye tsiku ndi tsiku, mlungu ndi mlungu mudzapeza chimwemwe choposa m'moyo wanu."

Kodi mungakonde kumuthokoza Yesu chifukwa cha mphatso yake ya mpumulo? Kodi mungakonde kumuthokoza lye chifukwa cha lonjezano la mpumulo wa chipulumutso tsiku liri lonse pokomana ndi zobetchera za moyo ndi lonjezano la mpumulo wa Sabata mlungu uli wonse polimbikitsa chiyanjano chanu ndi lye? Ngati simunachite choncho, kodi mungakonde kulandira chipulumutso chomwe amachipereka? Kodi mungakonde kumuza lye za chilako lako chanu chofuna kumasunga motere. "Inde Ambuye! Ndikufuna kupeza chimwemwe mu tsiku lomwe munalikhazikitsa." Bwanji osapanga chitsimikizo chotere tsopano lino?

CHINSINSI CHAKUKULA KUPYOLERA MUKUGAWANA

Larry ankasangalala ndi kukambirana kosangalatsa, kokhudzana ndi tiyi wa ku Japani, zakudya zophikidwa kuchokera ku mpunga, kunyumba kwa Komori, pamene alendo ena adayamba kutulutsa ma Baibulo awo. Onse adamuyang'ana iye ndi chiyembekezo."kodi mungatipatse mutu wa kukambirana kwathu lero? Amafunsa bambo Komori....

Larry anali pafupi kutsamwa ndi Tiyiyu.lye anaganiza kuti kucheza kwavo kudali kodzangosangalala limodzi basi. Ndipo panopa sanathe kupeza choti angagawane nawo anzakewo.

Larry adaphunzitsapo m'makalasi, mapunziro ambi amu Baibulo pa sukulu ina yophunzitsa chiyankhulo cha chingerezi ku Japan komwe anagwirako ntchito. Komanso onsewo ankayamba wawakonzekera kaye. Ankatha kuperekwa mapunzirowo mosavuta. Koma kuti angoyankhula mwadzidzi...zinali zosiyana.

Larry adamvapo nthano zonse zamu Baibulo kuyambira ali mwana. Koma sizinkatanthauza kanthu kwenikweni kwa iye payenkha. Ankachita zinthu zomwe iye ankadziwiratu kuti ndizolakwika pamaso pa Mulungu. Ndiye akadayankhula bwanji kwa ena za Mulungu yemwe iye mwini wake sanamudziwe?



Choncho, ali chikhaliye pa mpando wasofa, mozunguliridwa ndi anzake omuyembekeza aja, kuyerekeza kwake kudatsala pang'ono kutha. Nthawi yomweyo ali ndi mantha, vesi lamu Baibulo linafikira iye mumtima mwake lonena zamphamu ya mzimu woyera wotipatsa ife mau oti tinene tiri pakati pa anthu oti tiwachitire umboni (Luka 12:12). Adapezeka atayamba kulongosola nthano yomwe adaiganiza ya: mwana wolowerera.

Mmene analongosola momwe Mulungu amatikondera ife ngakhale ndi omwe asocherera kutari ndi iye, Larry adapezeka akulankhula zochokera pansi pa mtima wake. Mawu ake amanka natsikiratsikirabe kwa nthawi yoyamba m'moyo mwake, Larry adazindikira kuti Mulungu amamukonda iye kwambiri.

Usiku umenewo Larry adagwada pansi pa pakama wake naperekwa moyo wake kwa Mulungu yemwe pamapeto pake adakhala weni weni kwa iye. Kugawana zachikondi cha Mulungu zidapangitsa chinthu choposa kukhala wongodziwa zinsinsizo. Panopa sizidalinso nkhambakamwa ayi koma zenizeni zomuchenutsa iye.

1. YESU AKUTIBETCHERA KUTI TIKAKULE POGAWANA MAWU AKE

Ophunzira a Yesu adakhala zaka zitatu nditheka akuphunzira mawu a Khristu ndi kuona ntchito zake, komanso imfa yake ndi kuukanso kwake. Pamene Yesu anali pafupi kubwerera kumwamba, adawatuma ophunzirawo kuti akakhale akazembe ake.

"KOMATU MUDZALANDIRA MPHAMVU, Mzimu woyera atadza pa inu; ndipo mudzakhala mboni zanga m'Yerusalem... ndi kufikira malekezero ace a dziko." - Macitidwe 1:8.

Pamene otsatira ake a Yesu adali pa Pentekoste kuperekwa mitima yaho mosakayika kwa lye, Khristu woukitsidwayo adasimtha miyoyo yaho ndi mphamu za mzimu woyera. Adasandulika mboni, osati za

kuuka kwa ku thupi kwa Yesu Khristu ndi kukwera kwake kunka kumwamba kokha ayi, komanso za mphamvu zake za kuukitsa zomwe zidasintha miyoyo yawo.

Ife monga akhristu, ndifenso mboni ya pa zakuuka kwa Yesu chifukwa ife talandira ndi kuona nawo mphamvu yakusintha mwatsopano m'miyoyo yathuyi.

"Koma Mulungu wolemera cifundo, cifukwa ca cikondi cace cacikuru cimene anatikonda naco, tingakhale tinali akufa m'zolakwa zathu, anatipatsa moyo pamodzi ndi Khristu (muli opulumitsidwa ndi cisomo)...kuti akaonetsera m,nyengo zirinkudza cuma coposa ca cisomo cace, m'kukoma mtima kwa pa lye mwa Yesu Khristu."

- Aefeso 2:4-7.



Ife tapangidwa a moyo ndi Khristu kuti tikathe "kuonetsa chuma chosayerekezeka cha chisomo chake." Ndipo akutifunsa ife kuti tifalitsire uthenga wabwinowu, wa zomwe lye amachita m'moyo wamunthu, ku dziko lonse lapansi, ndikutilonjeza kunka nafe kulikonse kumene tikagwira ntchitoyi (Mateyu 28:19-20).

Munthu wina wotchedwa H.M.S. Richards, Yemwe adayambitsa utumiki wa Mawu a Chinenero wachinenero wa pa wailesi, adachitira umboni wotere nthawi ina:

"Ndaona kusintha m'mitima ya anthu amene anamva uthenga wa Yesu Khristu. Ndayenda m'malo m'mene dzina la Mulungu ndi la Khristu samadziwidwa mpaka pamene mpingo wake udatengerako uthengawu. Ndaona anthu akusintha kuchoka ku moyo wonyansa kupita ku moyo woyeru, kuchoka kumatenda kupita ku thanzi, kuchoka ku mantha wosatha a mizimu yoipa kunka ku chisangalalo cha chikhristu. Ndaona ine kusintha kwa amayi okhala m'banja. Ndaonanso mabanja a chikhristu enieni akuchoka ku moyo wachikunja. M'dela lirilonse limene ndayendako ndaona miyoyo ikusintha. Ndikudziwa kuti "uthenga wabwino wa Khristu... uli mphamvu ya Mulungu ya ku chipulumentso" (Aroma 1:16). Ndikudziwa kuti pamene mpingo ufalitsa uthengawu, kusintha kumachitika m'mitima ya anthu ndi mabanja awo, ndipo izi zimaonekera m'miyoyo ya awo amene avomereza kudandaauliraku."

Mulungu watipatsa ife anthu amene tiri ofoka mbali yapadera yoti tichite mu ntchito yake yokondweretsayi, chifukwa chakuti kugawana mawu ake iri mbali yofunika kwambiri mu kukula kwathu. Kuti chikhulupiriro chathu chikhalebe chabwino, chiyenera chionetsedwe. Monga anapezera Larry, mosayembekezera, kugawananso chikhulupiriro chathu kumatithandiza ife kuchita nacho mwathunthu, ndikutipangitsa ife kukula.

2. TIMAGAWANA ZA KHRISTU MU NJIRA YA M'MENE TIKHALIRA

Msungwana wina yemwe adakula mu banja la chizungu adapeza motere nthawi ina nati: "Ndidayang'ana makolo anga ndi zitsanzo zomwe anandionetsera zinandichotsa maganizo a umulungu; ndidalibenzo chitsanzo cha wina ali yense wa thupi la umutnuh yemwe adandikonda ine." Anthu otizungulira amasowa wina wake woti awapatse chithunzi chenicheni cha Mulungu. Akufuna wina wake wa "khungu ngati lawo" yemwe angawaonetse makhalidwe abwino. Ulaliki wamphamvu umene tingapereke ndi m'mene tikhala. Munthu asanafike posamala zomwe ukudziwa, ayenera kudziwa chisamaliro chomwe uli nacho. Petro akutiumiriza kuti:

"Ndipo mayendedwe anu mwa amitundu (osapemphera) akhale okoma,... akalemekeze Mulungu pakuona ntchito zanu zabwino m'tsiku la kuyang'anira. Pakutinso Khristu amamva zowawa m'malo mwanu, nakusiyirani citsanzo kuti mukalondole mapazi ake." - 1 Petro 2:12, 21.



Chifukwa "Khristu anazunzidwa" chifukwa cha ife pa Karivari, ife tsono tiri ndi chitsanzo cha chikondi chakudzipereka nsembe chomwe tiri nacho pafupi. Chikondi chimenecho, chinaonekeranso mwa ife pakukonda anzathu, ndipo chimasandulika mphamvu yoposa yosendezera anthu wosakhulupirira m'manja a Khristu.

3. TIMAGAWANA ZA KHRITSU MNJIRA IMENE TIMAGANIZIRA

Pamene mdierekezi anamuyesa Yesu m'chipululu muja ndi nkhanu yakufuna chakudya, kunyada ndi kungoganizira, Yesu adagonjetsa pogwirtsu ntchito mawu a m'bukhu lopatulika (Mateyu 4:4, 7, 10). Khristu anali atakonzekera ndi chifukwa anali atazama m'malembo oyera. Ndipo ndi m'menemo momwe nkondoyi inagonjetsedwera-m'mitima yathu.

"Pakuti monga asinkha (munthu) m'kati mwake, ali wotere; ati kwa iwe, idya numwe; koma mtima wace suli pa iwe." - Miyambo 23:7.

Akhristu omwe akukula amaganiza zakumwamba. Amaganizira kwambiri pa zabwino zomwe ayenera kuchita kuti afikirepo pachimake.

"Kondwerani mwa Ambuye nthawi zonse;... komatu m'zonse ndi pemphero, ndipembedzero, pamodzi ndi ciyamiko, zopempha zanu zidziwike kwa Mulungu. Ndipo mtendere wa Mulungu wakupambana cidziwitso conse udzasunge mitima yanu ndi maganizo anu mwa Khristu Yesu. Chotsalira, abale, zinthu ziri zonse zoona, ziri zonse zolemekezeka, ziri zonse zolungama, ziri zonse zoyeru, ziri zonse zokongola, ziri zonse zimveka zokoma; ngati kuli cokoma mtima cina, kapena citamando cina, zilingirireni izi. Zimenezonzo mudaziphunzira, ndikuzilandira, ndikuzimva, ndi kuziona mwa Ine, zomwezo citani, ndipo Mulungu wamtendere adzakhala pamodzi ndi inu." - AFILIPI 4:4-9.

Chomwe tidyetsa mtima ndi maganizo athu, chimatipangitsa kusinthika. Kaya muzoipa, zimatulutsanso zoipa. Kaya ndi mawu a Mulungu, amatulutsanso moyo waumulungu.

4. TIMAGAWANA ZA KHRISTU M'MAONEKEDWE ATHU

Monga kazembe wa Khristu, m'hristu ayenera kukhala wodzichepetsa kwa anthu onse kupewa makhalidwe ndi machitidwe onse osayenera.

"Momwemonso, akazi inu, mverani amuna anu ainu nokha kuti ngatinso ena samvera mau, akakondwe opanda mau mwa oyera ndi kuopa kwanu. Amene kukometsera kwanu kusakhale kwa kunja, kuluka tsitsi ndi kubvala za golidi kapena kuvala cobvala, koma kukhala munthu wobisika mumtima, m'cobvala cosaola ca mzimu wofatsa ndi wacete, ndiwo wamtengo wace wapatali pamaso pa Mulungu. Pakuti koteronso kale...(iwo) akuyembekezera Mulungu, anazikometsera okha, namvera amuna ao a iwo okha." - 1 Petro 3:1-5.

Kukhala mumavalidwe oyenera ndi zozikometsera zoyenera zimaonetsera chikhritsu chenicheni. Cholinga ndi choti, ena akopekere kwa ife ngati akhristu osati chifukwa chazomwe tiwauza za mavalidwe amakono, koma chifukwa cha zomwe maonekedwe athu a m'moyo akulankhulira kwa iwo za Yesu.



5. TIMAGAWANA ZA KHRISTU M'MACHITIDWE ATHU

Katswili wa mbiri zakale wotchedwa Edward Gibbon akutiua ife kuti pamene Galerius adagonjetsa asirikali achiperezi, thumba lodzala ndi ngale lidapezeka m'manja a msirikali wina wotenga zinthu wolanda. Mwamuna ameneyu adalisunga thumbali mosamala, natayamo ngalezo.

Anthu omwe amamatira ku zosangalatsa zomwe dziko lipereka-nakana za Yesu, ngale ya mtengo wapatali-ali pachoopsa choposa msirikali wakubayu. Simwayi wongotipeza kokha ayi komanso chipulumutso chamuyaya. Chotero Malembo oyera akutidzudzula kuti:

"Musakonde dziko lapansi, kapena za m'dziko lapansi. Ngati wina akonda dziko lapansi, chikondi cha Atate sichiri mwa iye. Pakuti chiri chosatha cha m'dziko lapansi, chilakolako chathupi ndi chilakolako cha maso, matamandidwe a moyo (kunyada) sidzichokera kwa Atate, ku dziko lapansi. Ndipo dziko lapansi lipita ndi chilakolako chache, koma iye amene achita chifuniro cha Mulungu akhale ku nthawi yonse." - 1 Yohane 2:15-17.



Satana akugwira ntchito yoopsa kuti adzetse tchimo loononga kwambiri ndi loipitsitsa. Olengeza za zakumwa zoledzeletsa amaonetsera achinyamata abwino, okongola, olimbika pa ntchito ndi okondwa. Sitinaoneponso womvetsa chisoni m'maonekedwe awo ngati yemwe adzandima ndi zoledzeretsa pochoka mu sitolo yomwela mowawo atanyamula thumba la zinthu m'dzanja lache.

Tiyenera kusamala ndi magulu omwe amaipsa Malamulo athu achikhritsu (2 Akorinto 6:14). Khristu, inde, akufuna tikafikire onse osapembedza. Ubale weniweni ndiwo umafalitsa ndi kugawa chikhulupiriro pakati pa wina ndi mzake. Inu mungoonetsetsa kuti magulu anu sali akukubwezeretsani inu ku zoipa zomwe mumachita kale mu moyo wanu. Zomwe titenga mmoyo wathu, ngakhale zokhudza chisangalalo, ziri ndi mbali yaikulu mu moyo wathu wachikhristu. Tiyenera kusamala pa zomwe tidyetsa maganizo athu.

"Sindidzaika chinthu choipa pamaso panga; chochita iwo akupatuka padera chindiipira." - Masalimo 10:3.

Ngati maganizo athu adzala ndi zabwino, zoipa sizingatikokere ife pansi. Poganizira mwakuya mu zinthu zomwe tingabweretse kunyumba ndi m'mitima yathu sizingachepetse miyoyo yathu. Mkhristu ali ndi zambiri zomupangitsa kukhala wokondwa kuposa wina ali yense.

"Mudzandidziwitsa njira ya moyo: Pankhope panu pali chimwemwe chokwanira; m'dzanja lanu la manja muli zokondweretsa zonka tuyaya." - Masalmo 16:11.

6. TIMAGAWANA ZA KHRISTU M'KUPEREKA KWATHU



Malemu M'busa H.M.S Richards, ali pafupi kubatiza wokhulupirira wina wake, adaona kuti munthuyo adali ndichikwama cha ndalamu zamapepala okhaokha m'thumba mwake. Mbusayu adamufunsa iye ngati mwina adaiwala kuchisiya polowa m'madzimo. "Chikwama changa ndi ine tibatizidwira pamodzi," munthuyo adayankha. Adali atapeza mzimu weniweni wachikhristu.

"Kupatsa ena mowathandiza. Akhristu amakula pakupereka, ndi chifukwa chake "Yesu adati:Nchodalitsa kupereka koposa kulandira" (macitidwe 20:35). Zomwe tipereka zokulitsa ufumu wa Mulungu zimabweretsa cholowa chosatha.

"Musadzikundikire nokha cuma padziko lapansi pamene njenjete ndi dzimbiri ziononga; ndi pamene mbala ziboola ndi kuba. Koma mudzikundikire nokha chuma m'mwamba... pakuti kumene kuli cuma cako, komwe udzakhala mtima wakonso." - Mateyu 6:19-21.

Pamene mupereka, kumbukirani: "Dziko lapansi ndi la Ambuye, ndi zonse zokhala m'menemo" (Masalmo 24:1), kuphatikizapo Siliva ndi golidi (Haggai 2:8). Tonse tiri a mwini wake Mulungu, chifukwa adatilenga ife ndikutipulumutsa kumachimo athu polipira dipo lamachimo athu ndi mwazi wake (Akorinto 6:19-20). Zonse zomwe tiri nazo ndizake za Yehova Mulungu chifukwa amatipatsa ife "mwayi wopezera chuma" (Deuteronomo 8:18).

Kodi Ambuye wathu wophedwa ndi woukitsidwa kwa akufayu akutiihana ife motani kuti tigawane naye popereka uthenga wabwinowo kwa ena?

"Kodi munthu adzalandza za Mulungu? Ndipo inu mundilanda ine. Koma mukuti, takulandani zotani? Limodzi limodzi la magawo khumi ndi zopereka... mubwere nalo limodzi lonse lakhumi, kunyumba yosungiramo kuti m'nyumba mwanga mukhale cakudya; ndipo mundiyese nako tsono ati Yehova wamakamu ngati sindikutsegulirani mazenera a kumwamba, ndikukutsanulirani mdalitso wakuti adzasoweka malo akuulandira." - Malaki 3:8-10.

Limodzi lakhumi "chachikhumi" cha "zoonjezera" zathu (Deuteromo 14:22; 14:22; Genesis 28:22). Kwa mlimi kapena wa Malonda, choonjezera kapena phindu ndicho chomwe chibwera pamwamba pazomwe tataya pogula zinthu zathu zantchito kwa wolembedwa ntchito, chimakhala malipro ake. Kupereka chachikhumi ndi lamulo lachikhaliwe chifukwa limakhudza khalidwe khalidwe. Polephera kupereka chachikhumi tima "mubera" Mulungu. Chachikhumi ndi cha Mulungu ndipo chiyenera kugwiritsidwa pa ntchito yokhayo yotumikira ntchito ya Khristu. (Akorinto 9:14), ndi kumalizitsa ntchito yake padziko lapansi kuti athe kubwera (Mateyu 24:24).



Pamene Yesu anadza kudzakhala nafe, anatipatsa chitsimikizo cha kupereka chachikhumi mu Chipangano Chatsopano (Mateyu 23:23). Kodi tiyenera kupereka zingati monga chopereka? Zopereka ziyenera kukhala monga mmene munthu woperekayo akuganizira. Munthu aliyense "apereke monga momwe mtima wake ufunitsa" (2 Akorinto 9:5-7). Simungapereke zoti muyeso wake wochulukitsa kwa Mulungu:

"Patsani, ndipo kudzapatsidwa kwa inu muyeso wabwino, wotsendereka, wokucumuka, wosefukira, anthu adzakupatsani m'maanja mwanu." - Luka 6:38.

H.M.S. Richards adayerekezapo nthawi ina izi ndi "Munthu wolanda moyo wake wonse yemwe adakhala naye pa msonkhano ku Los Angeles, ndipo sindidzaiwala nthawi imeneyi yomwe ndinkayankhula naye payekha paseri pa nyumba yochitiramo msonkhano. Adatulutsa m,ndandanda wa ngongole m,thumba lake zomwe zimakwana \$500, nandipatsa ine zonsez, nati, (ichi ndicho chachikhumi chomwe ndiyenera kupereka poyambirira."

Munthuyu sadali bwino ayi, ndipo ntchito yake idali kulanda ndi kuyenda juga kwa zaka pafupifupi makumi atatu kapena makumi anayi, ndipo ine ndidati, "kodi iwe tsono udzakhala bwanji ndi moyo?" "Iye adandiyankha, "ndatsala ndi ndalamwa zokwana zisanu ndi modzi za chi Amerika basi, koma inayonso ndi ya Mulungu."

"ndipo ndidafunsanso, "ndiye uchita bwanji?"

"sindikudziwa." Adayankha, koma ndidziwa kuti ndiyenera kupereka chachikhumi kwa Mulungu, ndipo iye adzandisamalira."

"ndipo Mulungu adamusamaliradi kulapa kwa munthuyu kudali koona. Adavula zonse ndi kudzipereka ndipo adakhala wokondwa mu moyo wake wonse wa chikhristu. Ndipo Mulungu adampatsa iye zonse

zosowa zake moyo wake wonse mpaka imfa." Mulungu sakulonjeza kuti Akhristu wokhulupirika onse adzakhala a chuma ayi, koma tiri ndi podalira pathu kuti Mlengi wathu adzatipatsa zosoweka mmoyo wathu.

Yesu anapereka zonse kwa ife. Tiyen'i nafenso tipereke mitima yathu kwa iye tsopano lino. Tiyen'i tigawire anzathu ena za Yesu kupyolera mu kakhalidwe, kaganizidwe, kaonekedwe, kachitidwe ndi kaperekedwe kathu. Bwanji osafufuza chimwemwechi chakugawana za Yesu ndi anzathu ndi ukulu m'chisomo chake chodabwitsachi?

CHINSINSI CHA MOYO WA THANZI

Akatswiri azofufuzafufuza azunzika ndi ntchito yawo kuti alembe zoonadi za zaka zomwe ziri mu Baibulo kuyambira pachiyambi: Anthu ali athunthu mu chipangidwe chakutumikira kwavo.



Chomwe ife tigawa kuti mwina chiru cha thupi, maganizo ndi uzimu pa munthu zimakhala zogwirizana ndipo zosalekanitsika. Mwa njira ina, tinganene kuti, chomwe chikhudza maganizo, chikhudzando thupi. Uzimu wathu umakhudzana ndi umunthu wathu ndiponso umunthuwu uli ndi mbali yaikulu pa uzimu wathu. Ife ndife anthu.

Mwachitsanzo, ofufuza motumbatumba amapeza kuti kukondwa, chimwemwe, kuseka zimapanga mu mphamu yachitetezo ya m'thupi la munthu. Mutha kuthandiza thupi kumenyana ndi matenda mokwanira pakungokhala wokondwa basi! Maphunziro awa amaonetsera mwapafupi thupi ndi maganizo zimagwirira ntcho pamodzi.

Zaka zikwi zapitazo Mawu a Mulungu adaonetsera kugwirizana kumene kulipo pakati pa maganizo ndi thupi zomwe ziri zovomerezekanso kwa malamulo a zachipatala.

"Mtima wosekerera uchiritsa bwino, koma mzimu wosweka uphwetsa mafupa." - Miyambo 17:22.

Molingana ndi zomwe Mtumwi Yohane, akufotokoza za mgwirizano wa maganizo ndi thupi ku Uzimu wathu.

"Wokondedwa, ndipemphera kuti pa zonse ulemere, nukhala bwino, monga mzimu wako ulemere." - 3 Yohane 2.

Mlengi wathu akufuna ife "Tikhale ndi umoyo wathanzi labwino." Mau a Mulungu atha kukhalanso kasupe wathu wathanzi, komanso wa moyo wosatha.

Popeza thupi ndi maganizo ndi uzimu wathu zimayendera pamodzi munchito zaho, Paulo akudandaulira motere:

"Chifukwa cace mungakhale mudya, mungakhale mumwa, mungakhale muchita kanthu kena , citani zonse ku ulemerero wa Mulungu." - 1 Akorito 10:31.

Uthengawu ukuphatikiza kubweretsa zonse za ku thupi ndi za Uzimu. Moyo wathanzi umathandiza ife kukhala akhristu amphamu ndi amachawi.

Pano pali njira zisanu ndi zitatu zoyenera kutsatilidwa pofuna kuthandiza kukhala ndi moyo wa thanzi komanso opambana.

1. MPWEYA WABWINO

Mpwuya wabwino ndi watsopano ndi ofunka pa thanzi kuti likhale labwino. M'nthawi ya tsiku komanso usiku pogona, mpweya wabwino m'nyumba zathu ndim'malo athu ogwirira ntchito uli wofunka kuti magazi athu athe kukhala ndi mbali ija yofunka ya mpweya (oxygen) kuti awutumize kumbali zonse za thupi. Kupumira mpweya wokwanira m'thupi lathu poyenda ndi njira imodzi yopambana kuti thupi likhale ndi mpweya okwanira.

Mpweya umene tipumira m'thupi uli wofunika koposa. Tiyeni tipewe kupumiramo mpweya womwe uli wosafunika komanso oononga. Kusuta kumaononga mpweya ndipo kumapha. Ofufuza motumbatumba apeza ndi kukhazikitsa mfundo yakuti kusuta fodya ndiko kumayambitsa matenda a m'mapapo a mtima ndi ena otero chilako lako cha fodya chikakhazikika zimavuta kuleka kusuta. Tisakokere mthupi mwathu mosasamala mpweya uli wonse woipa ndi zina zamajeremusi zoyambitsa matenda, kusuta fodya kumaononga mpweya ndipo ndi m'mene imfa zambiri zikubwerera chifukwa amapha. Azofufuzafufuza motumba apeza ndi kukhazikitsa mfundo yoti nthenda yam'mapapo imayambika chifukwa chosuta fodya, ndiponso kumayambitsa matenda a mtima ndinso kusokonezeaka kwa njira ya mpweya.

Thupi lozoloweretsedwa kusuta fodya limakhala lovuta kuti lidzasiye kusuta chifukwa mankhwala a ululu amufodyamo otchedwa "NIKOTINE" amapangitsa munthu kukhala wofuna kusuta nthawi zonse. Molingana ndi zotumbatumba Kusuta fodya kudzapha anthu zikwi zikwi khumi ndi ziwiri pa chaka mpaka kufikira m'chaka cha 2020 ngati anthu sasintha.

2. KUWALA KWA DZUWA

"Ubwino wa duwa ndi wambiri:

- (i) Kukhala padzuwa mphindi kuyambira khumi ndi zisanu mpaka makumi atatu m'mawa uliwonse kapena madzulo kumathandiza thupi kuti lithe kupanga ndi kugwiritsa ntchito lokha vitamin D; yemwe ali wofunika kwambiri ku khungu lathu. Ndipo amathandiza magazi kupanga Calcium ndi "Phosphorous" zomwe zimamanga ndi kulimbitsa mafupa athu.
- (ii) Dzuwa limakhalanso ngati lopha tizilombo toyambitsa matenda pakhungu monga Bacteria.
- (iii) Dzuwa limaperekwa mphamvu ku zomera zosinthira mpweya wa Carbon Dioxide ndi madzi kuti zikhale chakudya... popanda m'chitidwe umenewu, nyama ndi anthu zingathe kufa ndi njala
- (iv) Dzuwa limathandizanso munthu kuti athe kugwira bwino ntchito za usiku ndi kupuma ku zolemetsa zakubwera chifukwa cha usiku wautali wa nyengo za nthawi yozizira (yavuma).
- (v) Chenjezo duwa lithanso kukhala loipa. Kukhala nthawi yaitali kwambiri padzuwa kutha kuwaula khungu, ndi kuyambitsano matenda a pa khungu; kumakalambitsano msanga, ndiponso kumaononga maso ndi kuyambitsa ng'ala. (zonsezizikupezeza mu buku la zathanzi lotchedwa "Yang'ana Kumwamba kuti ukhale ndi Moyo" Iachingerezi) lomwe lidali Kotale wa maphumziro a Baibulo woyamba m'chaka cha 1993.



3. KUPUMULA

Thupi likuyenera kumapuma kuti lidzipangire lokha mobwezera momwe mwaonongeka. Tiyenera kukhala ndi nthawi yachisangalalo ndi kupuma kuti tipecukidwe ku zolemetsa za ntchito ndi mabanja. Popanda kupuma mokwanira, anthu amakhala olefuka, ndi osachedwa kunyasidewa ndi zochitika. Zoterezi zitha kuyambitsa matenda omwe amakhala ngati chotikakamiza kuti tibwezere kupuma komwe tidukukana kwa nthawi yaitali. Palibe choposa kupuma kwa usiku pogona.

Chinanso chofunika pa thanzi lathu ndiko kukonzanso moyo wathu wauzimu tsiku ndi tsiku. M'christu wochita nawo mawu a Mulungu tsiku ndi tsiku powerenga ndi kuphunzira ndi kupemphera adzachiza thupi lake ndi mzimu wake. Tiyeneranso ife kupuma ku ntchito zathu za nthawi ndi nthawi, pakupuma kamodzi tsiku lonse pa Mulungu, komanso pokhala ndi maholide a pachaka ndi pakati pachaka.

4. MACHITA CHITA OLIMBITSA THUPI



Machitachita olimbitsa thupi ali ofunika kwambiri ku thupi lathu motere:

- (i) "Amatithandiza kuteteza matenda a kuthamanga magazi.
- (ii) "Amathandiza magazi ambiri kuti afikire mbali zonse za thupi lathu, ndi kuti pali ponse pakhale pofundira.
- (iii) "Amathandiza kuchotsa zipsinjo za thupi ndi za maganizo zomwe; zimapangitsa kumva bwino moyo. Machitachita olimbitsa thupi ndiwo machiritso ku madandaulo ndi kuthodwa nkhawa.
- (iv) "Amatipatsa ife mphamvu ngati zamagetsi ku ubongo wathu ndi mbali zing'ono zing'ono za minyewa yathu, zomwe zimafiktsa paliponse poyenera zochitika zonse za m'thupi. Ndipo zimalimbitsa thanzi lathu politandiza mu mphamvu ya thupi yomenyana ndi kuteteza matenda. Thupi likakhala lochitachita masewera
- (v) olimbitsa thupi, maganizo amakhala ogwira bwino ntchito ndi achangu pogoniza zinthu zatsopano zabwino.
- (vi) "Amathandiza ku maonekedwe a thupi lanu ndi ku kusungani pa muyeso woyenera.
- (vii) "Amakupangitsani kukhala a mphamvu zoposa, kuti musamatopa pakugwira ntchito ngakhale pogoniza.
- (viii) "Amathandiza bongo kuti udzipanga mankhwala omwe amapangitsa umunthu wabwino ndi kuonjezera mphamvu yakuti muzitha kupirira ku zowawa. Ngati simunayambepo kuchita masewera olimbitsa thupi, yambani tsopano pang'ono pang'ono ndipo nkumaonjezera pang'ono nthawi iriyonse. Mutha kuwapeza a dotolo anu kuti akulangizeni musanayambe kupanga machitachita. Cholina chanu chikhale kuchita nawo masewero aliwonse olimbitsa thupi omwe angafanane ndi kuyenda mtunda umodzi kwa mphindi khumi ndi zisanu, kanayi kapena kuitirirapo pa Sabata iriyonse.

5. MADZI

Popeza madzi ndi ofunika kwambiri ku mbali iri yonse yochebetsetsa ya thupi lathu, tiyenera kumamwa kowirkiza.



"1. Pakulemera konse kwa thupi lathu, madzi ndiwo apanga mbali yayikulu pafupifupi maperesenti makumi asanu ndi awiri ndiwo madzi mthupi lathu.

"2. Thupi limafuna madzi osachepera mabotolo (malita) awiri patsiku kuti ligwire bwino ntchito zake zonse. Zina mwa ntchitozo ndizo kuyenda kwa magazi, kuchotsa zoipa m'thupi, kuyenda kwa chakudya ndi kugaya kwa chakudya.

"3. Munthu aliyense ali ndi pafupifupi zikwi zikwi pakati pa khumi ndi zisanu ndi makumi anayi za maselo (mbali zochepetsetsa zomwe zipanga) ku ubongo. Selo ina iri ndi pafupifupi maperesenti makumi asanu ndi awiri kapena asanu ndi atatu a madzi. Madzi okwanira ku maselo amenewa amathandiza kukhaziktsa maganizo abwino ndi oongoka kwa munthu, ndipo amateteza kukhumudwa ndi kukhudzidwa ndi zochitika monyansidwa.

"4. Simadzi okhawo omwe mumwa ali ofunika, kusamba madzi ozizira bwino tsiku ndi tsiku kumathandizanso, ku machitidwe a zoyendayenda mthupi; kupatsa mphamvu thupi ndi ubongo. Kusambakunso kumathandiza MINYEWA yomwe yosokonezeka, yomwe INGATHE kuyambitsa matenda popangitsa mphamvu yathupi yachitetezo kumatenda kukhala yoooka. Kusamba m'thupi kumachotsa zoipa zonse pa khungu ndipo kumachepetsa kutentha kwa thupi.

6. CHAKUDYA CHABWINO



Pachilengedwe, Mulungu adalangiza Adamu ndi Hava kuti adye mtedza, mtengo wakubala mbewu ndi therere, komanso zipatso (Genesis 1:29). Adamu ndi Hava atachimwa, masamba adaonjezeredwa ku chakudya chawo (Genesis 3:18) chitatha chigumula, Mlengiyo adaonjezera "Nyama yosadetsedwa" ku chakudya chawo (Genesis 7:2-3, 9:1-6).

Nyama ziri ndi mafuta ambiri komanso otchedwa "Cholesterol", omwe amaonjezera ngozi ya matenda aja akuthamanga kwa magazi kwakukuru, kufa kwa ziwalu za thupi, matenda a mitima, matenda a ndaka, kunenepa koipa, matenda a shuga ndi matenda ena ambiri. Lero lino, madotolo ambiri amalangiza iwo amene amadya nyama kuti achepetse madyedwewo, kapena aiphike bwino nyamayo ndi nsomba mosamalitsa.

Popeza anthu omwe amadya masamba okhaokha amakhala athanzi ndi a moyo wautali, akatswiri ambiri oona zachakudya ndi thanzi amatiumiriza ife kudya zomwe zidapatsidwa kwa makolo athu pachiyambi monga mtedza, mbeu ndi zipatso komanso kuonjezerapo masamba.

Ngati mufuna kuti mudzidya masamba, yambani mwaona ndi kudziwa mbali za chakudya chofunikira m'thupi zomwe zingapezeka popanda nyama. Idyani zipatso zosianasiyana kasanu kapena kasanu ndi kamodzi patsiku, komanso mtedza ndi mbewu, masamba ndi mtundu wonse wanyemba.

Masamba obiriwira komanso a chikasu, kuphatikizapo zipatso ndi zofunika kwambiri. gwiritsani ntchito ufa wa mtengo wakubala mbewu ndi mpunga womwe si woyerwa koma woderapo pachakudya chanu. Kudya zakudya zolimbitsa thupi zokhala ndi starichi kukhale kasanu ndi kamodzi kapena kuitirirapo patsiku. M'malo modya nyama ndi mafuta ake (monga "butter kirimu ndi zina) idyani mafuta a mtedza, chakudya tanenachi ndi chokwanira popanda nyama ngati mugwiritsanso ntchito zakudya zopangidwa ku mkaka.

Iwo amene asankha kudya nyama monga mbali yachakudya chawo, adye nyama zomwe Bukhu Lopatulika likuvomereza kuti ndi "Zoyerwa" kapena zoyenera pa munthu kuti zidyedwa. Pamene Mulungu adaloleza anthu kudya nyama, chitatha chigumula (Genesis 7:2-3) (Levitiko 11:47), adawauza nyama zake zomwe ziri zoyenera ndi zomwe ziri zosayenera kudyedwa.

Weregani mutu wa khumi ndi chimodzi wa Levitiko komanso wa khumi ndi chinayi wa Deuteronomo za mundandanda wa mbalame, nyama zamtchire ndi nsomba zomwe Mulungu adazitcha zoyenera kudyedwa. Potsatira mitu imeneyi, nyama zoyenera zikhale zogawanika ziboda ndi zobyikula. Nsomba zoyenera zikhale ndi mamba. Mbalame zodya nyama ndi zosayenera kudyedwa.

Mwa nyama zosayenera kuzidyazi, nkhumba ndiyo yomwe yatchulidwapo ndi kuletsedwa (Deuteronomo 14:8). Matupi ambiri a anthu aiptsidwa ndi matenda oopsa a nyongolosi zotchedwa "trichimae" nyongolosi zazing'onozi zimafalitsidwa kwa anthu podya nyama ya nkhumba. Chifukwa china chingakhale kuipa kwa kuchuluka kwa mafuta mu ziwalu zogaya chakudya za muthupi la munthu.

7. PEWANI ZINTHU ZAULULU

Kodi Baibulo likuchenjezanji pa zamowa (Kachasu)?

"Vinyo achita chiphwete, chakumwa chaukali chisokosa; wosochera nazo alibe nzeru." - Miyambo 20:1.



"Kapena ambala, kapena osirira, kapena oledzera, kapena olalatira, kapena olanda, sadzalowa ufumu wa Mulungu." - Akorito 6:10.

Kachaso (mankhwala aululu opezeka mu mowa) amasokoneza zochitika zofunika zathupi izi:

"1. Mphamvu yachitetezo cha mthupi - kachaso amachepepsa maselo a magazi oyera omwe amamenyana ndi matenda m'thupi, potero thupi limakhala pachoopsa chogwidwa ndi chibayo, chifuwa chachikulu, matenda a chiwindi, ndi matenda a ndaka a mitundu yosiyansiyana.

"2. Mphamvu yakupangitsa zochitika zonse za mthupi potulutsa zoyererera zache mthupimo. Kumwa kawiri kapena katatu kokha patsiku kwa zoledzeratsa kumapangitsa amayi kupita padera ngati ali oyembekezera, kubereka ana akufa kale, ndi kubereka nthawi isanakwane.

"3. Mphamvu ya kuyenda kwa magazi m'thupi lonse. Kumwa mowa kumaonjezera ngozi ya matenda a mitima, kuchepetsa shuga m'magazimo komanso kukweza mafuta m'magazi ndi kuthamanga kwa magazi, omwe ali matenda oopsa kwambiri.

"4. Kugaya kwa zakudya muthupi. Mowa umasokoneza m'mimba kupangitsa kuti idzitaya magazi. Kuchokera kukumwa mowa kumabweretsa mafuta m'chiwindi zomwe zimayambitsa matenda a chiwindi ambiri mbiri."

Mowa ndiwo umapangitsa anthu ambiri kudzipha okha, komanso kufa pa ngozi zapamsewu, kuzunza ana ndi nkhanza za pa nyumba.

8. KHULUPIRANI MU MPHAMVU YA MULUNGU

Munthu yemwe ali ndi mantha kapena atatsutsika saona phindu lakuchita zathanzi zomwe tanenazi. Koma munthu yemwe akusangalala m'chikhulupiro cha Mulungu moyenera adzapeza gwero leni-leni la umoyo wabwino:

"Lemekezani YEHOVA, moyo wanga ndi kusaiwala zokoma zache zonse atichitirazi: Amene akhululukira mphulupulu zake zonse; nachiritsa nthenda zako zonse. Amene aombola moyo wako ungaonongeke." - Masalimo 103:2-4.



Munthu wina wotchedwa Davide Larson, woona za anthu amisala ku chipata china ku America, adapanga kafukufuku wamkuru pazakugwirizana kwa Chikhristu ndi thanzi labwino. Kufufuza kwake kudaonetsera kuti zinthuzi ndi zogwirizana kwambiri. Anadabwanso kupeza kuti anthu omwe amapita kukapembeza ku kachisi amakhala moyo wautali kuposa omwe sapita, ndipo opita ku kachisiwa sagwidwa gwidwa ndi matenda ambiri a magazi ndi mtima ayi. Omwe akhulupira mwa Mulunguwa, amakhala moyo waphindu chifukwa sakhumudwa, kuti mpaka akayambe kumwa mowa, kapena kukhala m'ndende chifukwa cha kulakwira kawiri

kawiri kapena kukhala ndi banja losakondwa ayi kukhulupira mu mphamvu ya Mulungu yoyera ndilo khwerero lakukhala moyo wabwino, wathanzi ndi wokondwa.

Pafupifupi akhristu zikwi makumi asanu a chi Seventh-Day adafufuzidwa ku dziko la California, kwa zaka zoposa makuni atatu. Zotsatira zaka zinali zoti amuna a chi Adventist amakhala zaka pafupifupi zisanu ndi zinayi zoonjezera ndipo akazi, pafupifupi zaka zisanu ndi zitatu zoonjezera poyerekeza ndi amuna kapena akazi ena onse.

Zotsatira za ku Holland, Norway ndi Poland, zikusonyezanso chimodzimodzi. Ofufuzawa apeza kuti izi ziri chomwechi chifukwa cha mfundo za thanzi zomwe amuna ndi akazi ambiri a Seventh-day Adventist amatsatira, monga zomwe tanena mu phunziroli. Onse amene amatsatira mfundozi sangokhala kokha ndi moyo wautali ayi, komanso moyowo umakhala wabwino ndi wosiririka.

Kugwiritsa ntchito Baibulu ndi mau ake pa moyo wathu zikutisiyanitsa ife muzochitika zonse mudziko ndipo zimatipatsa njira zenizeni, zokhutitsa ndi umboni wakuti chikhristu ndi chipembedzo chenicheni, chofanizira m'zochitika m'dziko. Chimawasinta anthu - kupyolera m'maganizo komanso m'machitidwe awo- ndi kuwatengera ku moyo wamachitidwe atsopano.

Chifukwa cha kugwirizana kwa maganizo, thupi ndi moyo wathu wauzimu, Akhristu okhazikika ndi mau a Mulungu adzafuna kutsatira mfundo za moyo wa thanzi pamene akukonzekera kubweranso kwachiwiri kwa Yesu (Yohane 3:1-33). Khristu sangofuna kokha kuti tikonzekere kukumana naye pamene adzabweranso ayi. Koma akufunanso kupanga miyoyo yathu yaleroyi kukhala yabwino ndi yolongosoka. Tithe kugwirizana naye pa izi pongotsatira mfundo za moyo wa thanzizi.

Yesu akulonjeza kutimasula ife ku chizolowezi chakuchionongeko, kupyolera mu "Mphamvu yake yomwe iri pa ntchito mwa ife" (Aefeso 3:20). Ngati mukufuna kuthana ndi makhalidwe kapena zizolowezi zomwe zimaononga thupi monga kumwa mowa ndi kusuta fodya, thandizo lanu loposa la kusiya izi ndi kuitana mphamvu ya Mulungu yomwe imagwira ndipo ikugwira ntchito "Mwa Inu" Panokha simungathe. Mulungu atha kukupatsani mphamvu zogonjetsera. Mawu a Mulungu akulonjeza: "Nditha kuchita zonse mwa Khristu yemwe amandipatsa ine mphamvu" (Afilipi 4:13).

KULOWA MMOYO WACHIKHRISTU

Nayi kalata yopatsa chidwi yochokera kwa m'modzi wa ophunzira athu a Baibulo mu Afrika:

"Zaka zisanu zapitazo ndidalandira kalata ya pempho yochokera ku Mawu a Mzimu wa Chinenero kuti ndikayendere wa ndende wina yemwe amapanga nawo maphunziro a Baibulo pa makalata ndidaipereka kalata yopemphayo kwa akuluakulu oyan'ganira kundendeko omwe mwa chisomo adavomereza pempholo. Popeza kuti mphunziyu adali ndi chidwi kuphunzira Baibulo, ndinkamuchezera pafupi-pafupi.

"Patatha pafupi-fupi miyezi isanu ndi umodzi chiyambire kumuchezerera kuja, adafunsa kuti abatizidwe ndi kulowa mu mpingo. Oyang'anira ndende aja adapereka zipangizo za ubatizo kuti uchitikire mundende momwemo. Oyang'anira akaidi pamodzi ndi akaidi enanso adasonkhana kuchitira umboni umodzi mwa maubatizo opambana ndi osangalatsa omwe ndidabatizapo.

"Patangopita nthawi pang'ono chichitikire ubatizowo, mbaleyu adamasulidwa, ngakhalebe idali nthawi yake isadakwane yomasulidwa. Pamene ndidafunsa kuti izi zachitika bwanji, ndidauzidwa kuti moyo wake udasintha modabwitsa, ndipo adachitira umboni za Khristu Mpulumutsi wake ndi mpingo wake moti sanaonekenso ngati mkaidi, kapena kuchitiridwa ngati mmodzi wa iwo ayi. Munthuyu adalunzanitsidwa ndi banja lake moti panopa ndi mtsogoleri wa umodzi mwa mpingo yathu ikuluikulu"

1. KODI TANTHAUZO LA UBATIZO NDI CHIYANI?

Pamene wandendeyu adakhala Mkristu ndipo moyo wake nusinthika, ndi chifukwa chiyani kuti abatizidwe? Pokambiranwa ndi Nikodemo, mtsogoleri wa anthu anadza kwa Yesu usiku, ndipo Yesu namuonetsera poyeru kufunika ndi tanthauzo la ubatizo:

"Ngati munthu sabadwa mwatsopano, sakhoza kuona ufumu wa Mulungu... ngati munthu sabadwa mwa madzi ndi Mzimu, sakhoza kulowa ufumu wa Mulungu." - Yohane 3:3, 5.



Mukufotokoza kwake kwa Yesu tiyenera ife kubadwa "Mwa madzi ndi Mzimu". Kubadwa mwa Mzimu kumaimira kulowa moyo watsopano posinthika maganizo ndi mtima. Popeza kulowa ufumu wakumwamba kumafunika moyo wosinthika watsopanodi, osati moyo wakale wokhala ndi zigamba za makhalidwe osiyanasiyana ayi, ndipo uku kumatchedwa kubadwanso mwatsopano.

Ubatizo wa madzi ndi chionetsero cha kunja kwa thupi choonetsa kusinthika kwa m'kati. Wotiyimira wathu anabatiza wa ndende uja kusonyeza kudzipereka kwake kwa Kristu ndi chiyerekezero cha kusinthika komwe Mzimu woyeru udayambitsa m'khalidwe lake.

2. KODI NDIBATIZIDWE CHIFUKWA CHIYANI?

Chipulumutso chathu chimazungulira mu ntchito zazikuru zitatu za Khristu.

"Khristu anafera zoipa zathu monga mwa malembo;... anaikidwa; ndikuti anaukitsidwa tsiku lachitatu, monga mwa malembo." - Akorinto 15:3, 4.

Khristu anachipanga chipulumutso kukhala chotheka kupyolera mu imfa, kuikidwa mmanda ndi kuuka kwake kwa akufa.

"Kapena kodi simudziwa kuti ife tonse amene tinabatizidwa mwa Kristu Yesu tinabatizidwa mu imfa yache? Chifukwa chache tinaikidwa m'manda pamodzi ndi lye mwa ubatizo kulowa muimfa; kuti monga Kristu anaukitsidwa kwa akufa mwa ulemerero wa Atate, chotero ifenso tikayende m'moyo watsopano." - Aroma 6:3, 4.



Yesu adafera zochimwa zathu, naikidwa m'manda, ndipo nauka m'manda kutipatsa ife moyo watsopano wa chiyero. Tikabatizidwa timachita nawo mu imfa, kuikidwa ndi kuuka kwa Yesu. Ubatizo utanthonza kuti tafa ku uchimo, ndi Khristu kuika mmanda moyo wakale wa uchimo ndi Khristu ndipo mkuuka kukhala mmoyo watsopano mwa Khristu. Imfa ndi kuuka kwa Khristu ziri imfa ndi kuuka kwathunso. Mulungu angatipange ife kufa ku tchimo, ngati kuti tidapachikidwanso. Atha kutikhazikitsa ife amoyo ku zinthu za Uzimu, monga ngati kuti tauka kwa akufa. Ubatizo weni-weni umaimira makwerero akutembenuka. Choyamba, polowetsedwa mmadzi, kumizidwa kwathunthu, monga m'mene anthu akufa amatsitsidwira m'manda nakwiriridwa. Izi zikunena kuti ali olola kufa naye Yesu ndi kukwirira moyo wathu wakale. Ubatizo ndi maliro, kutsazikana ndi

khalidwe lomwe uchimo unalenga malo. Chachiwiri, timakwezedwa poturutsidwa m'madzi ndi uyo wobatizayo, monganso munthu woukitsidwa kwa akufa. Izi zikunena kuti ndife "cholengedwa chatsopano" choperkedweratu ku "Moyo watsopano" womwe Mulungu amatipatsa. Ndi kumizidwa kokha mmadzi komwe kungaperekere tanthauzo leni leni la ubatizo - kufa, kukwiriridwa ndi kubadwanso "Ubatizo" owaza madzi suli wokwanira kuimira kubadwanso mwatsopano, zimatanthauza chiyani kufa pamodzi ndi Khristuyo?

"Podziwa ichi, kuti umunthu wathu wakale unapachikidwa pamodzi ndi lye, kuti thupi la uchimo likaonongeke, kuti ife tisakhalenso akapolo a uchimo." - Aroma 6:6.

Ubatizo umaimira moonekera zomwe munthu ayenera kuchita m'kati kupereka zonse kwa Yesu. Tikasunga kena kake kubisila Mulungu, ndi chachidziwikire kuti tidzakhalabe mu "ukapolo wa tchimo". Pamene tidzipereka kwathunthu kwa Kristu, zilakolako zathu za uchimo zimasandulika "zopanda mphamvu," ndipo kusinthika kwathu kumayambika. Kodi yemwe amapangitsa kuti kusinthaku kuchitike ndani?

"Ndinapachikidwa ndi Khristu; koma ndiri ndi moyo wosatinso ine ai, koma Khristu ali ndi moyo mwa ine; koma moyo umene ndiri nao tsopano mthupi ndiri nao m'chikhulupiriro cha Mwana wa Mulungu, amene anandikonda, nadzipereka yekha chifukwa cha ine." - Agalatiya 2:20.

Ndikakhala mbali ya kupachikidwa kwa Khristu kupyolera mu ubatizo, ndimaitana mphamvu yaikuru m'moyo wanga. "Kristu amakhala mwa ine" Pofuna kuika moyo wanu kwathunthu mmanja mwa Khristu, choyamba muoneni Khristu akufa pa mtanda. Musayang'ane patchimo lomwe likukuopsezani, musayang'anenso moyo wanu wakale ndi kumva nawo chisoni; yang'anani kwa Yesu. Poona imfa yolimba mtima ndi yachisomo ya Yesu pa Karivale, mungathe kuonetsera kuvomereza kwanu ndi lye. "Mwa mphamvu ya mtanda ndikudzitenga kuti ndafa ku zizolowezi zoipa zakale ndikubvomera kwa Mulungu. Ndikupanga chitsimikizo changa ndi Kristu. Kuyambira tsopano kupita mtsogolo, ndidzakhala mwa chikhulupiriro mwa mwana wa Mulungu, yemwe adandikonda nandzipereka Yekha mmalo mwanga." Pamene tilawa mphamvu ya imfa ya Khristu ndi kuuka kwake timaona zambiri zaubwino wake zikulowa mmalo mwa zizolowezi zathu zakale zoipa.

"Chifukwa cace ngati munthu ali yense ali mwa Khristu ali wolengedwa watsopano, zinthu zakale zapita, taonani, zakhala zatsopano." - 2 Askorinto 5:17.

Kupyolera mu ubatizo, timaonetsera khumbo lathu logwirana manja ndi Yesu kuti tikakhale moyo watsopano ndi wabwino "Mwa Khristu." Yesu amatichitira ife zomwe ife tokha sittingathe kudzichitira. Timaturuka m'madzi cholengedwa chatsopano; lye amatipatsa mphamvu yokhalira moyo watsopano.

3. NDI CHIFUKWA CHIYANI YESU ANABATIZIDWA?

Pa tsiku la Pentekoste, Petro adawauza omwe amafuna kumasulidwa ku chitsutso kuti "mulape ndi kubatizidwa" kuti Khristu akukhululukire "zochimwa zanu" (Machitidwe 2:38). Popeza Yesu sadachimwepo m'kamodzi komwe, nanga adalola bwanji kuti abatizidwe?



"Pamenepo Yesu anachokera ku Galileya nadza ku Yordano kwa Yohane, kudzabatizidwa ndi lye,... kukwaniritsa chilungamo chonse motero." - Mateyu 3:13, 15.

Yesu adali wopanda tchimo. Adalibe choti alape koma adabatizidwa pa chifukwa china; "kukwaniritsa chilungamo chonse." Pobatizidwa, Yesu adaonetsa chitsanzo chabwino kwa ife anthu ofooka, ochimwa. Khristu sadafunsep omutsatira ake kupita komwe iye sadafikeko. Choncho pamene wokhulupirira amizidwa m'madzi aubatizo, akungotsatira m'mapazi a Mbuye wawo. Pakuti Kristu adafera machimo athu, athanso kutipatsa chilungamo chake.

"Ameneyo sanadziwa uchimo namuyesera ucimo m'malo mwathu; kuti ife tikhale chilungamo ca Mulungu mwa lye." - 2 Akorinto 5:21.


Kusinthidwa pamaso pa Mulungu kuchoka wochimwa kusandulika woyer, timakula kukhala "chilungamocco" potero timakhala moyo watsopano mwa Yesu.

4. NDI CHIFUKWA CHIYANI NDIYENERA KUMIZIDWA?

Khristu anamizidwa pa ubatizo wake, lye sadawazidwe madzi. Yohane adam'batiza lye mu mtsinje wa Yordano "chifukwa mudali madzi ambiri" (Yohane 3:23). pamene Yesu anabatizidwa, adalowa m'madzi ndipo "atangobatizidwa (kumizidwa) adaturuka m'madzi (Mateyu 3:16).

Tikamvetsetsa tanthauzo leni-leni la ubatizo, sitibvitikanso kudziwa mtundu weni weni waubatizo liwu lokhalo loti "ubatizo" linachoka ku chi Herene, liwu loti "Baptizo", kutanthauza kumiza (kulowa pansi). Pamene John Wesley amacheza ku Amerika mu chaka cha 1737, gulu la mpingo loweruza la anthu makumi atatu ndi anayi lidamupatsa mlandu chifukwa "chokana kubatiza mwana wa bambo Parker, ubatizo wina uliwonse woposa kumiza." Pali umboni woti tate wa mpingo wachi Methodist adabatiza otembenuka ake powamiza.

Wokonzanso John Calvin adati : "Ndichokhazikika ndithu kuti ubatizo womiza udayamba ndi mpingo wakalelo." - *Institute of the Christian Religion Bk 4 chapt. 15 Dec 19*. Mbiri ya mpingo wakale imaonetseratu poyer kuti ubatizo koma womiza. Dean Stanley, wa mpingo wa ku Mangalande, adalemba kuti, "Kwa zaka mazana khumi ndi anayi zojambirira, ubatizo wa dziko lonse udali womwe tawerenga mu Chipangano chatsopanochi, womwenso uli tanthauzo la " kubatiza" - kuti iwo omwe adabatizidwa, adalowetsedwa, kumizidwa m'madzi." - *Christian Institutions p. 21*.



Malo obatizira akhristu momiza akupezeza m'makachisi ambiri omwe adamangidwa pakati pa zaka za mazana anayi ndi mazana khumi ndi anayi ku Ulaya ndi ku Asiya, monga ku kachisi wamkulu wa ku Pisa, ku Italy ndi St. John, kachisi wamkuru kwambiri ku Roma. Kubatiza mowaza madzi kudayambika pamene khonsolo ya ku Ravenna ya mpingo wa katolika idavomereza kuwaza kuti ndi kofanana ndi kumiza mu zaka zoyambirira za mu zaka za mazana khumi ndi asanu.

Pochita za mpingo, sitiyenera kutsatira zomwe munthu ophunzitsa koma zomwe Khristu ndi atumwi ake akuphunzitsa. Akhristu ambiri oona mtima amatsatira mwambo wobatiza wana, ndi kuwapereka ana athu kwa Mulungu kuyambira pa chiyambi. Izi ndi zololeka. Komabe buku lopatulika, likuonetsera poyer a kuti munthu ayenera kuphunzitsidwa njira ya chipulumutso asadabatizidwe (Mateyu 28:19, 20) kuti munthu ayenera akhulupirire mwa Yesu asanabatizidwe (Machitidwe 8:35-38) ndikutinso munthu alape machimo ake ndi kukhululukidwa asanabatizidwe (Macitidwe 2:38).

Mwana wakhanda sangathe kukhulupirira, kulapa, kapena kuulula mphulupulu, zomwe ziyenera kuchitika munthu asanabatizidwe.

5. KODI NKOFUNIKA BWANJI KUBATIZIDWA?

Monga mwa kunena kwa Yesu, ubatizo ndi wofuniika kwa iwo ofuna kukalowa kumwamba:

"Ngati munthu sabadwa mwa madzi ndi Mzimu, sakhoza kulowa Ufumu wa Mulungu." - Yohane 3:5.

Yesu akungopereka chitsanzo chapadera. Mbala ya pamtanda ija idabadwa mwa Mzimu" ngakhale sadathe kuchoka pamtanda paja kuti akamizidwe mu ubatizo monga chizindikiro chakulapa kwake ndi kusintha mtima kwake. Ndipo Yesu adamulonjeza iye kukakhala naye mu Ufumu wake (Luka 23:42, 43). Kwa mbalayi, "kubadwa mwa madzi ndi Mzimu" kudaimiridwa ndi mwazi wa Yesu wokhet sedwa kumuyeretsa iye ku machimo ake.

Augustine adaonetsetsa mosamala, "kuti umboni umodzi basi wolementedwa wa kulapa uli pafupi kufa, ndiko kwa mbala ya pa mtanda, sizoti wina ataye mtima, chifukwa ndi yekhayo basi, palibenso."



Yesu adapereka chenjezo iri:

"Amene akhulupirira nabatizidwa, adzapulumutsidwa; koma amene sakhalupirira adzalangidwa." - Marko 16:16.

Pofa mmalo mwathu pa Karivari, Yesu adaonetsera poyer a chikondi chake pa ife. Tiyenera kubvomerezano poyer a, polapa mopanda kuchita manyazi za kudzipereka kwathu kwa Khristu mu ubatizo. Kodi mwayamba moyo watsopano mwa Yesu Khristu? Kodi mwabatizidwa? Ngati siziri choncho, bwanji wosakonzekera kuti mudzabatizidwe m'tsogolomo?

6. UBATIZO NDICHO CHIYAMBI CHABE

Ubatizo umaimira kudzipereka kwathu ku moyo wa chi Khristu. Koma kudzipereka kwathu ku ubatizo sikukhala nthawi zonse. Mwana akabadwa, kumakhala kofunika kusangalala, tsiku lobadwa likadutsa ndi chisangalalo chija chitha, mwanayo amafunika kudya tsiku ndi tsiku, kusamba, ndi kumuchitira zofunika zake zonse tsiku ndi tsiku. Ndi chomwechonso ndi ubatizo.

Paulo ananena motere pa zomwe adakumana nazo, "Ndimafa tsiku ndi tsiku" (1 Akorinto 15:31). Mwa kubwerera kuchoka ku kudzikonda tsiku ndi tsiku, timakhala tikuyankha moyenera kwa Khristu moonjezera. Mwambo wa ubatizo, monganso wa ukwati



woyera, zaikidwa kukhala chitsimikizo kuti ubale wayambika ndi wokula. Kuti ubalewo ukulebe kosalekeza, tiyenera kudzipereka tokha tsiku ndi tsiku kwa Khristu, kalandira moyo watsopano tsiku ndi tsiku mwakupemphera ndi kuphunzira Baibulo.

7. CHIFUKWA CHOSANGALALIRA

Ubatizo uyenera kukhala chifukwa chosangalalira, chifukwa omwe aika chikhulupiro mwa Yesu ali ndi chiyembekezo cha moyo wosatha. "Yense amene akhulupirira nabatizidwa adzapulumutsidwa" (Marko 16:16). Pamene tibatizidwa, tiri pa ulendo wokwera kunka ku chikondwerero chosatha.

Ubatizo ndi chikondwerero cha chimwemwechi cha lero ndi Yesu. Iye akulonjeza mphatso yaulele ya Mzimu woyera kwa iwo obatizidwa (Machitidwe 2:38). Mzimu umadza ndi zipatso za Mzimu "Chikondi," chomwe chimadzaza moyo ndi "kufatsa, chifundo, ubwino, kukhulupirika, kudekha ndi kudziletsa" (Agalatiya 5:22-23).

Kukhala ndi Yesu ife mwa Mzimu wake woyera kumatipatsa chikhaliidwe cheni-cheni chakuya. Popezanso Mzimuyo mwini achitira izi umboni... kuti ife tiri ana a Mulungu" (Aroma 8:15,16). Ubale wathu wotetezedwa pakati pathu ndi Mulungu umatibweretsera ife zabwino zambiri, koma sichtsimikizo kuti sitingakumane ndi mabvuto ayi. Ndiponsotu, mdaniyo amayesetsa nthawi zambiri kubweretsa mavuto ochuruka kwa iwo amene angodzipereka kumene kwa Khristu.

Komabe, ngati tilumikizana manja athu ndi a Mulungu, tidzadziwa kuti lye atha kugwiritsa ntchito chiru chomwe lye akufuna kwa ife kuti chichitike, chabwino ngakhale choipa, kutipulumutsa ndi kutithandiza kuti tikule (werengani Aroma 8:28).

Mayi wina wachisungwana adapanga chitsimikizo choti apereke moyo wake kwa Khristu ndi kubatizidwa ngakhale mwamuna wake adamuwopseza kuti amuleka ukwati akangochita zimenezo. Bambo samafunafuna mpangono pomwe kusya chikhulupiro chake, chatsopanocho komabe anaumirira kwa Yesu nakhala wachikondi chachikuru kuonetsera kwa mamuna wake. Koposa kale kwa kanthawi, mwamunayu anayesetsa kumapanga zinthu zoti mayiyu azivutika pakhomopo. Koma pamapeto pake adagonja pa mafunso omwe sadathe kuyankha. Kusinthika kwa moyo wa mayiyu. Mwamunayu adaupereka moyo wake kwa Yesu ndipo nayenso adabatizidwa.

Kuumirira chifupi ndi Yesu Khristu "mu nthawi zowawitsa ndi zokoma" kudzatipanga ife kukhala zida zamphamu m'manja mwake. Titha kuipereka miyoyo yathu kwa lye mopanda kukaikira chifukwa lye adadzipereka kale kwa ife pamene adalipira dipo laulere la machimo athu pa mtanda paja. Mwayitu nanga uwu wakuti tikanene poyer, kumupatsa lye chikondi chathu ndi kumumvera lye! Ngati simunachite kale izi, bwanji osatero tsopano. Mufunseni lye kuti akulengereni moyo watsopano mwa inu mwa mphamu ya Mzimu woyera, ndi kuti mubatizidwa mwa Khristu.

CHINSINSI CHA KUKULA KUPYOLERA MU CHIYANJANO

Kumayambiro a zaka za 1960, mbale Andrew, mwamuna wochokera ku Holland, m'dziko la Romania kudutsa oyang'anira a chi "Communist" pa chipatapo. Adakapeza malo okhala ku Hotela nayamba kupemphera kuti Mulungu amutsogolere iye ku gulu loyenera la Chikhristu-limene lingathe kugwiritsa bwino ntchito ma Baibulo omwe adabweretsawo.

Kumapeto a Sabata imeneyo, Andrew adapita kwa kalaliki wa mu Hotelayo namufunsa za komwe angathe kukapeza Kachisi.

Kalalikiyo adamuyang'ana iye mwachilendo namuyakha kuti, "Tiribe anthu ambiri otero kuno, iwenso ukudziwa. Pambali pa izi, iwenso siutha chiyankhulidwe chakuno".

"Kodi sudadziwe eti?" adayankha Andrew,

"Akhristu amayankhula chiyankhulo chimodzi."

"Ooh! Ndiye chiti chimenecho?" "Chimatchedwa Agape"(chikondi chopanda malire).

Kalalikiyu adali asadamvepo za izi, koma Andrew adamutsimikizira iye nati "Ndicho chiyankhulo chabwino koposa padziko lonse lapansi.

Andrew adatha kupeza mipingo ingapo m, deralo natha kukumana ndi wamkulu ndi mlembi wa mpingo wina wake, Mwatsoka, ngakhale Andrew ndi amunawa adatha kuyankhula ndi kumva ziyankhulo zingapo za ku Ulaya, adapeza kuti mwa ziyankhulo zonsezoo, padalibe chomwe amatha kumvana. Ndiye adangokhala nkumangoyang'anana wina ndi m'nzache. Andrew adali atayenda mitunda yambiri yoopsa ndi katundu wake wamtengo wapataliyu, koma sadatha kupeza ngati amuna awa omwe adakumana nawo adalidi akhristu eni eni abale kapena akazitape (azondi) a Boma. Pamapeto pake adapeza Baibulo lachiyankhulo cha chi Romania chakumeneko. Ndipo Andrew adatulutsa Baibulo lachiyankhulo cha chi Dutch nthumba lake.

Adavundukula pa 1 Akorinto 16:20. Nalisiya chomwecho, naloza pa dzina la bukhulo lomwe adatha kulizindikira. Nthawi yomweyo nkhopo za anthuwo zidawala. Mwachangu anapeza mutu womwewo ndi vesi lake mu ma Baibulo awo achiyankhulo cha Chi Romania nawerenga: "Abale onse kuno akupereka moni. Mupatsane moni ndi kupsopsona koyer."

Anthuwo adawalira pa Andrew, ndipo wina wa iwo adapeza mu Baibulo lake pa Miyambo 25:25 ndipo Andrew adalipeza vesili nawerenga: "Monga madzi ku moyo wothodwa ndiwo Mau a Uthenga Wabwino kudziko lachilendo."

Anthuwa adakhala theka la ora kukambirana ndi kugawana za m' Mawu a M'Baibulo basi, Adali okondwa kwambiri mukugawanaku mwakuti padalibenzo kusankhana ziyankhulo ndi zikhulupiriro ndipo adafika poseka chikhakhaza kufikira misozi idaturuka m'maso mwawo.

Andrew adadziwa kuti wapeza abale ake. Pamene adawaonetsa iwo katundu wa ma Baibulo aja, anthu a ku Romania awa adakondwera koposa namukumbatira mobwerezwa bwereza.



Usiku umenewo, ku Hotelayi, kalaliki uja adapita kwa Andrew nati, Nena, ndayang'ana tanthauzo la liwo loti "Agape" mu bukuhamatantu a mawu. Palibe chilankhulo cha mtundu umenewo. Ili, koma, ndi liwu la mu chi Herene lotanthauza Chikondi."

Andrew adamuyankha nati, "Ndi choncho ndithu. Ndinayankhula m'chomwechi masana onse."

Kodi mwapeza chilankhulo chabwinochi? Mu phunziro iri, muphunzira za m'mene Mulungu angatibweretsere tonse pa bwalo lake limodzi lalikuklu la chikondi.

1. MPINGO WOKHAZIKITSIDWIRA KUKUMANIRA PAMODZI

Yesu adakhazikitsa mpingo ndi cholinga chokwaniritsa chofunika pa munthu kuti asamalidwe ndi kuthandizidwa. Tonse tiri ndi zosowa. Ndicho cholinga cha mpingo. Iwo ndi malo omwe timayanjana ndi kuthandizana wina ndi muzake. Mau opatulika akutivumbulutsira za mpingo waukulu wa atumwi omwe udatana amuna ndi akazi kukapempedzera limodzi mokondwa kufikira mpaka kwa wamphamu zonsezo.

"Chimene tidachiona, ndipo tidachimva, tikulalikirani inunso mukayanjane pamodzi ndi ife, ndipo chiyanjano chathu chirinso ndi Atate, ndipo ndi mwana wake Yesu Khristu; ndipo izi tilemba ife, kuti chimwemwe chathu chikakwaniridwe." - Yohane 1:3, 4.

Gulu la anthu lomangika pamodzi ndi mitima yaho kupolyera mukulumikizana ndi Yesu komanso ndi wina ndi m'nzake, limapeza "Chisangalalo" chathunthu! Onse amayankhula chiyankhulo chimodzi chiyankhulo cha chikondi.

Akhristu amakhala mbali imodzi ya banja losefukira. Amakhala abale ndi alongo mwa Khristu popeza onse amakhala ndi mzimu umodzi wapfuko limodzi. Pamene mgwirizano waterowu ukula niukhala ndi anthu ambiri, mphamu za m'gwirizanowu zimakhalanso zolimba pakati pa a Khristu.

Ziwalo za mpingo wokhazikitsidwa atumwi, ndi atumwi a Yesu, udamangika pamodzi mwazikhulupiriro zofanana, chikondi chawo pa Mulungu, ndi kukhumba kwavo kumutumikira lye ndi kugawira ena za Chisomo Chake ku dziko lapansi. Kulumikizana kwenikweni uku kwa kupembedzera pamodzi kudali chifukwa chimodzi chomwe chidapangitsa kuti mtundu uwu wa anthu ochepe, opanda mphamu ndi ozunzidwa ndi kuphedwa ulitembenuze dziko chadodolido.

2. MPINGO WOMWE KHRISU ADAKHAZIKITSA

Kodi Khristu ali ndi mpingo? Kapena cholinga cha kukhala ndi gulu kapena bungwe lachipembedzo chidali chifuniro cha munthu? Yesu akuyankha:

"Ndipo pa thanthwe ili ndidzakhazikitsa mpingo wanga, ndipo makomo a dziko la a kufa sadzaulaka uwo." - Mateyu 16:18.



Yesu ndiye thanthwe lokhazikika, mwala wapangodya, wa Mpingo wake.

Kodi ndi gulu lotani lomwe linapanga mbali ya maziko?

Omangika pa maziko a a tumwi ndi aneneri, pali Khristu Yesu mwini, mwala wa pangodya." - Aefeso 2:20.

Yesu Ambuye adakwaniritsa chiyani pamene uthenga udalalikidwa?

"Ndipo Ambuye anawaonjezera tsiku ndi tsiku amene akuti apulumutsidwe." - Machitidwe 2:47.

Pamene Yesu adakhazikitsa mpingo, adalonjeza kuti "Makomo a gehena sadzaulaka uwo" (Mateyu 16:18), ndipo mpingo wa Khristu upirirabe chipiririre. Wakhala uli ndi adani amphanmvu - kuyambira maufumu a Roma kufikira ku olamuliro ankhanza wa komunisiti - koma mwazi wa iwo omwe adafera uthengawu udapangitsa mpingowu kukula ndi mphamvu. Pamene wopembedza m'modzi anatenthedwa kapena naponyedwa ku mikango, ena ambiri adauka kulowa m'malo mwake. Akaligwiritsa adayesetsa kuchinyonyosola chipembedzo cha chikhristu. Koma choonadi cha chikhristu chapikisana nawo bwino lomwe kuposa kale mu mbadwo wa sayansi ndi chikunja.

Chobetchera chachikuru chimodzi cha Mpingo chidadza pamene udaloledwa ndi boma la Aroma kukhala chipembedzo chodziwika mu ufumuwu. Mpingo udakula mopambana - koma pampapeto pake udaipitsidwa. Udaoneka wakufa mu uzimu mu nthawi ychedwa ya mdima (Dark Ages). Koma Ambuye adasunga nthawi zonse Akhristu olimba mtima ndi okhulupirika omwe mu nthawi yamavuto ndi yowawitsa, adaonetserabe kuwala ngati nyenyezi mu usiku wopanda mwezi.

Paulo akuyerekezera ubale wa a Khristu ku Mpingo wake ndi chiyanjano cha mwamuna chakuteteza mosamalitsa mkazi wake (Aefeso 5:23-25). Mpingo ndi banja, ndipo chiwalo chiru chonse chiru kukhazikitsa ubale weni weni ndi chiwalo chinzake cha m;banjalo, ku chitapo kanthu mu zonse zothandiza pa banjalo (Aefeso 2:19).

Paulo akuyerekezerano mpingo ngati thupi, ndi Khristu mwini wake ngati mutu wake (Akolose 1:18).

Pamene tabatizidwa, timaonetsera poyeru ku chikhulupiriro chathu mwa Yesu ndi kukhala ziwalu za "thupi", mpingo.

"Pakutinso mwa Mzimu m'modzi, ife tonse tinabatizidwa kulowa m'thupi limodzi." - 1 Akorito 12:13.

Bukhu la Chibvumbulutso likutionetsera Khristu woukitsidwa akuyenda pakati pa miping, kuyionetsera chisamaliro chake (Chibvumbulutso 1:20, 12, 13). Khristu sanawasiyepo anthu ake okha, ndipo sadzatero ayi.

3. MPINGO WA CHOLINGA

Kupita kukapembedza kumpingo m'chofunika kwa Mkhristu. Timasowa thandizo la ena kuti chikhulupiriro chathu chikhalebe chamoyo ndi kukula.

Mpingo uli ndi zofunika zitatu izi:

(1) Mpingo umasamalira choonadi.

Monga "Mwala wa maziko wa choonadi" (!Timoteo 3:15). Mpingo umagwiriziza ndi kuteteza choonadi cha Mulungu padziko lapansi: Tiyenera ife nzeru zamgwirizano za anthu opembedza kuti zitithandize ife kuona choonadi chenicheni chofunika cha m'malembo oyera.

(2) Mpingo uli chitsanzo cha zomwe chisomo cha Mulungu chimachitira munthu wochimwa.

Kusintha komwe Khristu amachititsa m'miyoyo ya anthu okhulupirira kumachitira umboni za Mulungu yemwe amatitchula ife kutiitanira "Mukuwala kwake kozizwitsa" (1 Petro 2:9).

(3) Anthu ake a Mulungu ali mboni zake ku dziko lonse ndi zosowa zake. Yesu asanabwerere kunka kumwamba, lye adawalonjeza akuphunzira ake:

"Koma mudzalandira mphamvu, Mzimu Woyera atadza pa inu: Ndipo



mudzakhala mboni zanga M'Yerusalemu, ndi M'Yudeya lonse, ndi m'Samariya, ndi kufikira malekezero ace a dziko." - Machitidwe 1:8.

Ndi mwayi waukuru kuti Mpingo utengere uthenga wa chikondi chachikuru cha Mulungu kudziko lonse lapansi.

4. WOKHAZIKIDWA KUTI UKHALE NDI MPHAMVU

Mpingo womwe Khristu adakhazikitsa udali ndi dongosolo lolozeka. Munthu amatha kulowetsedwa, komanso kuchotsedwa monga Chiwalo cha Mpingo (Matenu 18:15-18). Mpingo wa Mulungu umasankha atsogoleri ndipo unali ndi likulu lake padzikolo lino komanso malo ang'onoan'gono okomanirako (Machitidwe 8:14; 14:23, 15:2; 1 Timoteo 3:1-13) Pamene adabatizidwa, okhulupirirawo amalowa gulu lokhazikitsidwa mwadongosolo (Machitidwe 2:41 ndi 47).

Mpingo uli ndi cholinga cha kulimbikitsana

"Ndipo tiganizirane wina ndi mzache kuti tifulumizane ku chikondano ndi ntchito zabwino, osaleka kusonkhana kwathu pamodzi, monga amachita ena, komatu tidandaulirane, ndiko koposa monga momwe muona tsiku (lakudza Khristu) lirikuyandika." - Ahebri 10:24, 25.

Izi, mwachidule, ndizo zomwe gulu la mpingo wathanzi umachita ziwalo zake zimakulitsana m'chikhulupiriro, ndi kulimbikitsana. Mulungu adalinganiza mpingo wake kuti ulimbikitse anthu a Mulunguyo ndi kutumikiranso dziko lapansi. Titha kuchita zambiri ndi zoposa m'chigulu kusiyana ndi pamene tichita mwatokha. Tangoonani inu chitsanzo chimodzi chokha.

Mpingo wosunga Sabata moyembekezera kudzanso kwachiwiri kwa Khristu (Seventh-Day Adventist): Timafalitsa uthenga wabwino kupyolera mu ntchito zachipatala padzikolo lonse lapansi -kugwiritsa ntchito zipatala zoyenda m'magalimoto m'mizinda ikuuiukulu ndi m'midzi ndi zipatala zing'onozing'ono m'midzi yokhala kwaokha kapena zisumbu kumwera kwa Pacific. Masukulu athu abweretsera makumi azikwi za achinyamata ku chidziwitso cha moyo wabwino mwa Khristu - kuyambira ku sukulu yaukachenjede yaikulu ya Loma Linda, komwe amaphunzitsa ngakhale ntchito ya madotolo yakusintha chiwalo cha mtima mwa munthu; kufikira ku timasukulu ting'onoting'ono tachimishoni tomwe tawanda mkatı monse mwa Afirika.



Koma timalimbana ndi ngozi ndi njala popereka chithandizo kupyolera mu bungwe la ADRA. Mipingo ing'onoing'ono ikudyetsa anthu ndi kuwapatsa zovala ovutika ndi opanda pokhala mu malo zikwi zikwi a chithandizowa. Ndipo magulu ambirimbiri osiyanasiyana a chi Adventist akugawira uthenga uwu wachipulumutso mu maiko osachepera mazana awiri. Ndigulu lokhalo lokhazikitsidwa mwa dongosolo lokhala ndi a Khristu odzipereka lomwe lingathe kuhala ndi chikoka chokhudza dziko lonse motere.

Khristu ndi atumwi adayerekezera mpingo ndi thupi, nalongsola kuti ziwalo zonse za thupi ndi zofunika (a Akorinto 12:21-28). Ziwalo zonse zathupi sizofanana ayi, koma zonse ziri zofunika kwambiri ndipo ziyanera kugwirira ntchito pamodzi mogwirizana.

Diso lomwe lachotsedwa pa thupi silingaone. Mkono wolekanitsidwa ndi thupi ulibe ntchito. Kaya ife ndife diso kapena mkono, kapena chala, sitingakhale otakataka mwa phindu pa za Khristu pa tokha ayi.

Kuhala chiwalo cha mpingo, kulumikizitsidwa ku ziwalo zina za thupi, kumatipatsa ife mphamvu monga a Khristu.

5. THE JOY OF WORSHIP

Chimwemwe cha kupembedza. Mkatikati mwa mitima yathu muli chikhumbo khumbo chopembedza Mulungu, ndipo chikhumbo khumbo ichi chitha kufota ngati sitichionetsera. Kodi wolemba Masalimo adamva bwanji poganzira za kupita ku malo opembedzera?

"Ndinakondwera m'mene ananena nane tiyeni ku nyumba ya Yehova." - Masalimo 122:1.

Kodi nyimbo ziri ndi mbali yanji pakupembedza pagulu?

"Tumikira Yehova ndi chikondwerero: Idzani pamaso pake ndi kumyimbira mokondwera." - Masalimo 100:2.

Baibulo likutiua ife kuti kupereka zopereka ndi mbali inanso yoyenera ya kupembedza koyeria.

"Bwerani nacho chopereka, ndipo fikani ku mabwalo ace. Gwadirani Yehova woyeria ndi mokometsetsa." - Masalmo 96:8-9.

Pemphero lirinso chofunikira chachikuru chakupembedza kwa pagulu.

"Tiyeni, tipembedze tiverame, tigwade pamaso pa Yehova, amene anatilenga." - Masalmo 95:6.

Kuphunzira Baibulo ndi kulalikira ziri mbali za pa chilikati penipeni pa chipembedzo cha m'chipangano Chatsopano. Kuyambira pa ulaliki wa Petro pa tsiku la Pentekoste, wopezeka mu Machitidwe 2, komanso kuyambira munthawi ya otsutsa okonzanso kuti choonadi chisasokanezeke kufikira m;masiku athu ano, chitsitsimutso chirichonse cha uzimu cha chipembedzo chagonera pa kulalikira za mu Baibulo. Nanga ndi chifukwa chiyani? Ndichifukwa chakuti "Mawu a Mulungu ndi a moyo ndi akuchitachita. Akuthwa kuposa lupanga lakuthwa konsekone" (Ahebri 4:12-13).

6. CHOYENERA NDI CHITI NDI MPINGO?

Ena amatsutsa zoti mpingo wadzala ndi anthu osalungama. Koma zomwe munthu wina wochedwa Henry Kland Beecher adanena ndi zonna zoti, "Mipingo simalo oonetsera anthu woyeria okhaokha ayi, koma uli Sukulu yakuphunzitsa osayenerawo kukhala oyenera."

Popeza palibe m'modzi waife amene ali wangwi, Mpingo sudzakhalanso wangwi. Yesu, mmafanizo ake, limodzi la iwo likutikumbutsa kuti nansongole ndi tirigu zimakulira pamodzi (Mateyu 13:24-30). Tikaverenga m'Chipangano Chatsopano, m'makalata a Paulo, tipeza kuti mpingo wa atumwi udali ndi mabvuto oopsa. Ndiponso mpingo wa lero uli ndi zilema zake. Koma, chonde, kumbukirani kuti palibe mpingo wa zifukwa umene ungaononge kapena kujejemetsa mwala wa pangodya wa mpingo - Yesu Khristu mwini. Tsuno, mu Mpingo wathu wosakhala ndi anthu angwirowo tiyenera kulunjika maso pa Mpulumutsi yemwe amatitumikira. Pambali pazovutozo, Mpingo uli wa mwini wake Yesu, ndiye yanga'nirani pa Khristu.

"Khristu anakonda Eklesia (Mpingo) nadzipereka yekha m'malo mwace kuti akampatule, atamyeretsa ndi kumsambitsa madzi ndi mawu; kuti iye akadziikire yekha Eklesia wa ulemerero, wopanda banga kapena khwinya, kapena kanthu kotere; komatu kuti akhale woyeria, ndi wopanda chilema." - Aefeso 5:25-27.



Mpingo ndi wofunika kwambiri kwa Yesu koteru kuti "Adadzipereka yekha chifukwa cha Mpingo " pamene adafera munthu wina aliyense payekhapayekha ndi mpingo wonse pamodzi. Chotero kukhala ziwalo za mpingo zikhale zofunikiranso kwa inu. Kodi ndinu chiwalo cha thupi la Khristu?

7. KUPEZA MPINGO

Kodi ndi zipembedzo zonna zingati zomwe Yesu ali nazo pa dziko lapasi?

"Thupi limodzi ndi Mzimu umodzi,... Ambuye mmodzi, chikhulupiro chimodzi, ubatizo umodzi." - Aefeso 4:4, 5.

Popeza Khristu ali ndi "Chikhulupiro chimodzi" chokha basi, nanga tingachidziwe bwanji? Yesu akutipatsa ife mfungulo wake wopezera:

"Ngati munthu ali yense afuna kuchita chifuniro chake (Mulungu), adzazindikira za chimphunzitscho, ngati chichokera kwa Mulungu, kapena ndilankhula zochokera kwa ine ndekha." - Yohane 7:17. (onaninso pa Yohane 8:31, 32).



Pamene tipanga chitsimikizo kuchita chifuniro cha Mulungu, lye adzatithandiza kuona ngati chiphunzitscho chiri chochokera kwa lye kapena chiri chopangidwa ndi mwambo wa munthu,. Pofuna kupeza mpingo woyenera, tiyenera kuyesa kumvera kwake ku Mawu a Mulungu, chagonera pa Mawu a Mulungu, osati pa mtsogoleri wamphamvu wa mpingowo kapenanso kukula kwa mpingo ayi.

Pitirizani kufufuza mu maphunziro athuwa yendani m'kuunika pamene Mulungu akuvumbulutsira kwa inu kuchokera m'Bukhu Lopatulika, ndipo adzaonetsera momveka bwino cholinga chake pa inu

Mkhristu yemwe akukula ndi munthu amene atsegula mtima ndi maganizo ake kalandira choonadi monga m'mene Mulungu akuchivumbulutsira kuchokera Mawu ake.

KODI GULU LINGAKHALE LOLAKWA

Mu phunziro lathu lakhumi ndi chisanu ndi chimodzi, tidapeza kuti kuchita nawo mpumulo wa Sabata ndi chinthu chofunika kwambiri ku moyo wathu wopsinjika wa masiku ano. Popeza Mulungu amatimvetsetsa ndi chosowa chathu chiri chonse, adakhazikitsa tsiku lachisanu ndi chiwiri lonse kuti tikapumule ku ntchito zathu zakuthupi ndi kutitsitsimutsa mu uzimu. Atatha kulenga dziko lathu lapansi lonse kwa masiku asanu ndi limodzi, lye "adapumula" pa tsiku lachisanu ndi chiwiri, "ndi" kuliyeretsa" tsikuli (Genesis 2:1-3).

Pamene Mulungu adapereka malamulo khumi kwa anthu ake, a Israyeli, lye adaika lamulo losunga tsiku lachisanu ndi chiwiri monga Sabata ngati chirikati chenicheni cha Malamulo onse (Eksodo 20:8-11). Molingana ndi lamulo limeneli, Sabata ndi lokumbutsa mphamu ya Mulungu yakulenga, tsiku lakukhala chete ndi kuganizira kukongola ndi zozizwitsa za ntchito ya chilengedwe chake, tsiku lotakasuka ndi kudza pafupi ndi Mlenji wathu, tsiku lofufuza mwakuya za mbale wathu ndi lye wotilengayo.

M'moyo wa munthu wa Yesu padziko lapansi, Iyenso adasunga Sabata (Luka 4:16) nalitsimikiza kuti liri tsiku lakupindulitsa a Khristu (Marko 2:27, 29). Mavesi ambiri a m'bukhu la Machitidwe akuonetsera poyer molongosola bwino kuti ophunzira ake a Yesu adapembedza pa tsiku la Sabata Yesu atangouka kwa akufa (Machitidwe 13:14; 16:13; 17:2; 18:1-4, 11).



1. FUNSO LOSOKONEZA NDI LOBVUTA

Izi zikutibweretsa ife ku mutu umene anthu ambiri amaona ngati wovuta ndi wosokoneza. Akhristu padziko lonse lapansi akhala kwa nthawi yaitali akupembedza masiku awiri olekana. Mbali inayi, Akhristu ambiri akupempedza tsiku loyamba la pa Mulungu (Sunday), limene akulikhulupirira kuti likumbutsa kuukanso kwa akufa kwa Khristu. Kwinanso, gulu lina lalikulu, loona mtima ngati loyambadi, limakhulupirira kuti Bukhu Lopatulika limazindikira Sabata la pa tsiku lachisanu ndi chiwiri lokha basi ndipo palibe paliponse pamene pakuonetsa kupatulidwa kwa tsiku loyamba la pa Mulungu

Kodi pali kusiyana pakupembedza tsiku lirilonse lomwe munthu afuna ngati Sabata? Monga anthu oona ndi a chilungamo omwe afuna kudziwa choonadi, tiyenera kumadzifunsa nthawi zonse tokha: "Chofunika kwa Yesu ndi chiyani? Kodi Yesu akufuna kuti ine ndichite chiyani?"

Pofika pa chitsimikizo cha Funsoli, mfundu zambiri zofunika ziyenera kulongosoledwa momveka bwino: Adasinta tsiku la Sabata lenileni ndi ndani kulibweretsa ku tsiku loyamba la pa Mulungu? Kodi Baibulo likuvomereza kusinthaku? Ngati ndi choncho, Mulungu kapena Yesu, kapena atumwi ndiwo adapangitsa kusinthaku?,

Tipitirira pakuona za mafunso onsewa ngati ali otheka.

2. KODI MULUNGU ADALISINTHA TSIKULI?

Kodi palipo pamene Mulungu adalengeza kuti wasintha tsiku la Sabata kuchoka ku tsiku la chisanu ndi chiwiri kupita ku tsiku loyamba la pa mulungu?

Akhristu ambiri amavomereza za Malamulo khumi a Mulungu monga chowatsogolera choyenera kukhalira m'moyo, polemba ndi chala chake,



kwa mtundu wa anthu. Ali ofunika kwambiri adawalemba iwo pa magome a miyala ndi chala chake (Eksodo 31:18).

Mu lamulo lachinayi Mulungu akutilangiza kuti:

"Uzikumbukira tsiku la Sabata likhale lopatulika. Masiku asanu ndi limodzi uzigwira, ndi kumariza ntchito zako zonse; koma tsiku lachisanu ndi chiwiri ndilo Sabata la YEHOVA MULUNGU WAKO; usagwire ntchito iri yonse... chifukwa masiku asanu ndi limodzi Yehova adamariza zakumwamba ndi zapansi, ndi nyanja, ndi zinthu zonse ziri m'menemo, napumula. Tsiku lachisanu ndi chiwiri; chifukwa chache Yehova ANALIDALITSA tsiku la Sabata kuti likhale LOPATULIKA." - Eksodo 20:8-11.

Pamene Mulungu adapereka Malamulo Khumi kwa anthu ake, adaonetseranso poyer a kwa iwo kuti munhu ayenera abwerezze ndi kulembanso Malamulowa ochokera ndi pakamwa pake Mulunguyo poyer a.

'MUSAMAONJEZA pa mau amene ndikuuzani, kapena KUCHOTSAPO, kuti musunge Malamulo a Yehova Mulungu wanu, amene ndikuuzani." - Deuteronomo 4:2.

Mulungu mwini akulonjeza kuti sadzasintha Malamulo ake:

"Sindidzaipsa chipangano changa, kapena kusintha mau oturuka m'milomo yanga." - Masalimo 89:34.

Baibulo liri lomveka bwino kuti Mulungu sadasinthe Sabata kuchoka ku tsiku lachisanu ndi chiwiri kupita ku tsiku loyamba la pa mulungu.

3. NANGA KODI KAPENA YESU NDI YEMWE ADASINTHA SABATA?

Molingana ndi Yesu, Malamulo khumi sasintha:



"Musaganize kuti ndinadza Ine kudzapasula chilamulo kapena aneneri: Sindinadza kupasula, koma kukwaniritsa. Pakuti indetu ndinena kwa inu, kufikira litapitirira thambo ndi dziko, kalemba kakang'ono kamodzi kapena kansonga kake kamodzi sikadzachokera kuchilamulo, kufikira zitachitidwa zonse." - Mateyu 5:17, 18.

Mu phunziro lachikhumi ndi chisanu ndi chimodzi, tidapeza kuti chidali chizolowezi cha Yesu kukapembedza ku sinagoge pa tsiku la Sabata (Luka 4:16). Tidapezanso kuti Yesu adafuna kuti ophunzira ake apitirize chisangalalo cha kusunga Sabata koona (Mateyu 24:20).

Zikuonetsera poyer a kupyola mu ziphunzitso za Yesu ndi zitsanzo zake kuti ifebe tikufunika Sabata la kupuma, kutakasuka, ndi kuhala nayo nthawi ndi Mulungu wathu.

4. KODI NANGA ATUMWI NDIWO ADASINTHA SABATA?

Yakobo, mtsogoleri woyamba wa mpingo wa mpingo woyambirira wa a Khristu, adalemba zokhudzana ndi Malamulo khumi:

"Pakuti aliyense angasunge Malamulo onse, koma akakhumudwa pa limodzi, iyeyu wachimwira onse. Pakuti lye wakuti 'Usachite chigololo', anatinso 'Usaphe'. Ndipo ukapanda kuchita chigololo, koma ukapha, wakhala wolakwira lamulo." - Yakobo 2:10, 11.



Luka, sing'anga ndi Mlaliki wa uthenga mu mpingo woyambirira, adati:

"Tsiku la Sabata tinaturuka ku mudzi kunka ku mbali ya mtsinje, kumene tinaganizira kuti amapempherako; ndipo tinakhala pansi ndi kulankhula ndi akazi amene adasokhana." - Machitidwe 16:13.

Chipangano Chatsopano, m'buku la Machitidwe mukunenedwa za kupembedza Sabata pafupifupi kwa nthawi makumi asanu ndi atatu mphambu zinayi. Akunenawo ndiwo otsatira ake a Khristu, onse pamodzi okhalako kuposera pa zaka khumi ndi zinayi, kuyambira pamene Yesu adauka kwa akufa: MASABATA awiri ku Antiokeya (Machitidwe 14:14, 42, 44); Sabata imodzi ku Afilipi (Machitidwe 15:13); Masabata atatu ku Atesalonika (machitidwe 17:2-3); Masabata makumi asanu ndi awiri mphambu zisanu ndi zitatu ku Akorinto (Machitidwe 18:11).

Yohane, womaliza kufa mwa atumwi khumi ndi awiri aja, adasunga Sabata. Ndipo adalemba kuti:

"Ndinagwidwa ndi Mzimu tsikula Ambuye." - Chibvumbulutso 1:10.

Malingana ndi Yesu, tsiku la Ambuye ndilo Sabata.

"Pakuti Mwana wa Munthu ali mwini tsiku la Sabata." - Mateyu 12:8.

Kufufuza umboni m'malembo oyera kwavumbulutsa kuti atumwi sadayeserepo kusintha tsiku la Mulungu la kupuma kuchokera ku tsiku lachisanu ndi chiwiri kupita nalo ku tsiku loyamba la pa mulungu. Chipangano Chatsopano chikutchula tsiku loyamba la pa mulungu maulendo asanu ndi atatu basi. Monsemo sadaonetsemo kuti liri tsiku loyera kapena kuti liyenera kupatulidwa ngati tsiku lopembedza ayi. Kufufuza bwino bwino mwakuya ndi moganizira mosamalitsa za mavesi asanu ndi atatuwa anena za tsiku loyamba la pa mulungu tiona kuti tsikuli lidali ndi zochitika izi:

- (1) Akazi adadza kumanda patsiku loyamba la pa mulungu (Mateyu 28:1).
- (2) "Pamene Sabata linadutsa," akazi adaptiriza ntchito zavo pa tsiku loyamba lapa mulungu (Mariko 16:1, 2).
- (3) Yesu adaonekera koyamba kwa Mariya wa Magadala mawa wa tsiku loyamba lapa mulungu (Marko 16:9).
- (4) Otsatira a Yesu adaptiriza ntchito zavo pa tsiku loyamba lapa mulungu (Luka 24:1).
- (5) Mariya adaptita ku manda a Yesu napeza m'manda muli mbee! Patsiku loyamba la pamulungu (Yohane 20:1).
- (6) Akuphunzira a Yesu adasonkhana pamodzi "poopa Ayuda" (osati kudzapembedza ayi) pa tsiku loyamba lopa mulungu (Yohane 20:19).
- (7) Paulo adapempha ziwalo za mpingo kuwerengera chuma chawo patsiku loyamba lapa mulungu, ndi "Kupatula ndarama zina" za osanka ku Yerusalem (1 Akorito 16:1, 2). Sikunenapo zakukumanira kwa mpingo kupembedza ayi.
- (8) Pa Machitidwe 20:7, Luka akunenapo za kulalikira kwa Paulo pa tsiku loyamba la pamulungu pa msonkhano wapadera wochitikira chifukwa cha kutsazikana ndi abale. Zoonadi Paulo adalalikira, koma iyeyu adali kulalikira tsiku ndi tsiku, ndipo atumwi anali kunyema mkate tsiku ndi tsiku (Machitidwe 2:45).

Palibe vesi lirilonse mwa awa likuonetsera kuti atumwi adaganizapo zoleka kusunga Sabata la tsiku lachisanu ndi chiwiri. Atumwi sadatchulepo zakusintha kuchokera ku tsiku lachisanu ndi chiwiri kupita ku tsiku loyamba lapamulungu. Palibiretu umboni uli wonse mu Chipangano Chatsopano chonse pa zakusinthaku. Kusintha kudadza atatha masiku a Yesu ndi atumwi, choncho tiyenera kubwerera ku mbiri kuti tione kuti zinasintha liti, ndipo zimasintha bwanji:

5. KODI (SUNDAY), TSIKU LOYAMBA LA PAMULUNGU LIDABWERA BWANJI?

Aneneri akutichenjeza momveka bwino kuti Akhristu ena adzasiya zikhulupiro zoona za , "chipangangano Chatsopano cha Ukhristu: "Chotero, chenjerani!" (Machitidwe 20:29-31). Ndipo izi ndizomwe zidachitikadi oona za mbiri mwakuya adalembe za m'mene Akhristu adayambira kutayana ndi chiyero cha utumwi.

Zikhulupiro zachikunja miyambo zikhulupiro za uzimu zomwe Paulo, Petro ndi ena omwe adayamba ntchitoyi ya mpingo wa Mulungu sizidapeza njira ina iri yonse yolowera mu Mpingo.

Kusintha kwakusunga Sabata loona kupita ku kusunga tsiku loyamba lapamulungu kudachitika chitatha Chipangano Chatsopano, atumwi onse atafa. Mbiri ikufotozoa kuti a Khristu tsono adayamba pang'ono ndi pang'ono kuchoka ku chipembedzo choona ndi mpumulo wa Sabata wa pa tsiku lachisanu ndi chiwiri la pamulungu ndi kuyamba kusunga tsiku loyamba lapamulungu.

Komabe sikuti okhulupirira adasiyiratu kusunga Sabata loona ayi ndikupitiratu ku Sabata la chilendoli monga tsiku la Ambuye. Chiyambi chenicheni cha kusiiratu chidali ku dziko la Italy, mkatikati mwa zaka za mazana awiri atafa Khristu. Kwa nthawi yaitali kuchokera pamenepa a Khristu akhala akusunga masiku onse awiri wa pamene enanso akupangabe Sabata loona basi.



Pa 7 Malichi, m'chaka cha A.D. 321, Konsitantini wamkuru adaika lamulo lakupembedza tsiku loyamba lapa mulungu kuti likhale Sabata, kuwakakamiza anthu onse, kupatulapo alimi,aku Roma, kuti azipuma pa tsiku loyambali lamuloli, kuphatikizapo ena asanu omwe Konsitantini adakhazikitsa okhudzana ndi tsiku loyamba lapa mulungu, udapangitsa tsikuli kukhala lokhazikika ndi lamulo kuyambira nthawi imeneyo mpakana lero.

Muzaka za mazana anayi, Bungwe la Lodikaya lidaletsa a Khristu kuti asamasiye kugwira ntchito zaho pa tsiku la Sabata loona, ndi kuwaumiriza kusunga tsiku loyambali lapamulungu posagwira ntchito

iri yonse ngati kudali kotheka.

Mbiri ikutisoneyenza kuti kupembedza pa tsiku loyamba ndi kutsatira lamulo la munthu. Bukhu Lopatulika silikuvomereza kupembeza pa tsiku loyamba la pa mulungu.

M'neneri Daniel adalosera kuti m'nthawi ya chi Khristu, kudzabwera mphamvu yakunyenga yoyesera kusintha Malamulo a Mulungu (Daniel 7:25).

6. ADASINTHA IZI NDANI?


Kodi ndi ndani adalichotsa Sabata ku tsiku lachisanu ndi chiwiri kupita ku tsiku loyamba lapamulungu? Mpingo wa Katolika umavomereza kuti ndiwo udasintha izi. Adachita izi pofuna kupumitsa ufumu wa Roma womwe munthawiyi unapasuka, kufikira kuti atsogoleri a mpingo adakambiranu ndi kugwirizana kusintha tsiku lakupembedza kuchoka ku lachisanu ndi chiwiri kupita ku loyamba lapamulungu.

Katekisima wa mpingo wa katolika amati:

"FUNSO: Kodi tsiku la Sabata ndi liti?

"YANKHO: Tsiku lachisanu ndi chiwiri (Saturday).

"FUNSO: Nanga ndi chifukwa chiyani timapembedza pa tsiku loyamba la pa mulungu (Sunday)?



"YANKHO:Timasunga tsikuli m'malo mwa lachisanu ndi chiwiri chifukwa Mpingo wa Katolika... udalisintha choncho." Wolemba, Peter Geirmann. (Zopezeka mu Katekisima wa zikhulupiro za a Katolika wa 1957, tsamba 50.)

Mpingo wa Katolika umalengeza monyadira kuti atsogoleri a mpingo wa anthu adasintha chotere.

"Tsiku loyera, Sabata, lidasinthidwa chotere- osati motsogozedwa ndi mawu a m'malembo opatulika ayi koma mwa mphamvu yomwe mpingo udaziona kuti uli naz... Anthu omwe akuona kuti udindo wonse wa zinthu ngati izi wagonera pa mawu a Mulungu, malemba ake oyera, ayenera kukhala ziwalo za mpingo wa "Seventh-day Adventist", ndi kusunga Sabata loona, kukhala "Loyer" (Zonenedwa ndi Cardinal Maida Bishop wamkuru wa ku mpingo wa Katolika wa Catherine woyera ku Detroit, Algonac, Michigan, May 21, 1995).

7. NANGA MIPINGO INA YA MPATUKO IKUTIPO CHIYANI?

Zolembra zokhazikitsidwa zoonetsa zikhulupiro za mipingi ingapo yamipatuko zikugwirizana ndi kunena kuti Baibulo silinapereke udindo wakusintha kuti anthu adzipembedza pa tsiku loyamba lapamlungu.

Martin Luther, yemwe adayambitsa mpingo wa chi "Lutheran", adalemba mkulapa kwake kuti: "Iwo (mpingo wa Katoloka) akunena kuti Sabata lidasintha kuchokera kutsiku lachisano ndi chiwiri kupita ku tsiku loyamba lapamlungu, tsiku la Ambuye, kusempha na ndi (Malamulo Khumi)... ndipo palibe chomwe amachinyadira koposa ngati kusintha uku komwe adakupanga kukhala kotheka. Iwonso akunena modzikweza kuti, mphamvu yawo ndi yaikuru koposa ya utsogoleri wa mpingo wawo, chifukwa idatha kusintha limodzi la Malamulo Khumi a Mulungu." (Augsbury Compession, Arbele 28, paragraph 9.)

Woona za chipembedzo m'maphunziro a chi "Methodist", Amos Binney ndi Daniel Steele adaona izi: "Ndi zonna, palibe chochitira umboni ubatizo wa ana akhanda.... Kapena kusunga tsiku loyamba lapamlungu monga Sabata." (Theological Compend New York: Methodist Book Concern, 1902) tsamba 180, 181.

Dr, N Summerbell, woona za mbiri ya ophunzira a Yesu Khristu kapena mpingo wake, adalemba: "Mpingo wachi Roma udapatutsa kwathunthu... udasintha lamulo lachinayi la Mulungu pochotsa Sabata la Mawu a Mulungu, ndi kuikapo Sabata lawo la patsiku loyamba lapamlungu kukhala loyera" - (A Time Ministry of the Christian and the Christain Church, tsamba 417, 418).

8. KODI NKHANI YAIKURU APA NDI ITI?

Mutu uwu ukutibweretsa maso ndi maso kuti: Ndichifukwa chiyani anthu ambiri achi Khristu akupembedza patsiku loyamba lapamlungu limene Baibulo silimavomereza? Chofunikiranso kuposa apa, ndi tsiku liti lomwe ndiyenera kulisunga? Kodi nditsatire awo akuti" palibe kusiyana pa tsiku lomwe munthu asankha kupembedza bola ngati ndikusunga limodzi pa mlungu"? kapena/ iwo amene akuti; Kodi ndisunge kukhala tsiku lomwe Yesu, Mlengi wathu, pamene a malenga dziko lathu lapansi , ndi tsiku lomwe Mulungu adalionetsera m'malamulo ake khumi: tsiku lachisanu ndi chiwiri kukhala Sabata?"

Apa tikulimbana ndi zoposa kusunga kuonetsera kunja koma nkhanu ndi yoti, kodi tsiku lenileni loonekera kuti liri lenileni mu Baibulo ndi liti? Nkhani yaikuru apo ndi kumumvera Yesu. Mlengi wathu adaptatula Sabata monga tsiku loyera", nthawi yathu ndi mabanja athu kuti tidze chifupi ndi lye kupezako mphamvu ndi chitsitsimutso. Kodi ndimvere yani? Ndimvere Khristu, Mwana wa Mulungu, kapena miyambo ya munthu pa za tsiku loyenera kulisunga kukhala loyera? Chisankho ndichoonekeratu poyer:



Ziphunzitso za anthu kapena lamulo la Mulungu. Mawu a munthu kapena Mawu a Mulungu. Munthu wolowa m'malo kapena lamulo loyera.

Mneneri Daniel akuchenjeza kolimba kwa iwo akuyesera "Kusintha nthawi zoikika ndi chilamulo" (Daniel 7:25) "Kapena ofuna kusintha nthawi ndi chilamulo" (Daniel 7:25). Mulungu akuitanira anthu ake kuti abwere kwa lye.. Akuwaitanira iwo ku kusunga Sabata ngati chizindikiro cha kumvera ndi chikondi chawo pa lye.

Yesu anati, "Ngati mukonda lne, sungani Malamulo anga" (Yohane 14:15). Ndipo akulonjeza chisangalalo chathunthu kwa iwo akumukonda, lye ali nafe chidwi kuti tipeze chikondi chake chathunthu. Mtima wa munthu wofuna kumvera umatheka kutseguka mokwanira ku chikondi chimenechi.

M'munda wa Getsemane, Khristu adadzipereka kwathunthu ku chifuniro cha Atate wake - ngakhale adakomana nawo mtanda ndikuti machimo a dziko lonse adachotsa moyo wake. Pamene analirira kwa Mulungu, "Chikho ichi chindipitire" adakhalabe wodzipereka mkudandaula kwake, ndi adatinso, "Koma osati monga mwa kufuna kwanga ayi, koma kufuna kwanu" (Marko 14:36).

Khristu akufuna ife tikapeze chikwaniritso chomwe moyo wodzipereka moona umabweretsa. Ndiponso lye akufuna kuti ife tikapeze chisangalalo cha mpumulo wa Sabata. Lye akufuna ife kuti timukhulupirire ndi kumudalira lye kwathunthu pomumvera mu zochitika zonse za m'moyo. Ngati mubvomereza kuitana kwa Mulungu uku ndi kumumvera pa Malamulo ake onse, mudzalandira lonjezo la Yesu loti mtendere wake udzakhala "wa inu" ndipo "chisangalalo chanu" chidzakhala "chathunthu" (Yohane 15:11).

KODI MULUNGU NDI WACHILUNGAMO

M'nyamata wina waphedwa ndi mfuti akulemba ntchito yake yakusukulu pagome lakunyumba mkaati mwa mzinda wina.

Mayi wachichepera mu dela la mzinda wina wapeza kuti mwana wake ali ndi matenda a Edzi chifukwa cha magazi oonongeka ndi matendawa omwe iye analandira kuchipatala atadwala.

Mavuto a matsokawa a kunka nachulukira-chulukirabe m'dziko lathu lapansili. Ndipo tikufuna yankho la zonsezi. Kodi Mulungu amakhala ali kuti m'dziko la mavuto ndi imfa? Wolemba Masalimo akutitsimikizira ife kuti "Dziko ladzala ndi chikondi chake cha Mulungu chosalephera" (Masalimo 33:5).

Koma ngati izi ziri zoona, ndi chifukwa chiyani lye sathetsa kunzunzika ndi matsokawa? Mutu wamakumi awiri wa Chivumbulutso ukutionetsera m'mene Mulungu adzathetsere tchimo ndi mazunzo komanso nthawi yake ya zonsezi.



1. ZAKA CHIKWI ZIVUNDUKULIDWA M'KUSATHULA

Mutu wa Makumi awiri wa Chivumbulutso ukulongsola momaliziratu za zaka chikwi zotsatira pa kubweranso kwa Khristu. Zochitika za m'zaka zimenezi zidzakhala zomaliza mu mkangano wa Satana ndi Khristu womwe wakhalako kuyambira pamene tchimo linalowa m'dziko.

Zonsezi zinayambira kumwamba pamene Lusifara anachita nsanje ndi Khristu, nayamba nkondo ndi angelo osagonjetsedwawo, naponyedwa kuchokera kumwamba kudza ku dziko lapansi. Izi zinapitirira pa dziko lapansi m'munda wa Edeni, mpaka pamene zinafika pa chimake choyamba pomwe Mdierekezi anakopa anthu kuti am'pachike Yesu. (Mutha kuwerenganso izi mu phunziro lathu la chitatu lija). Zochitikazi zidzafika pachimake chomaliza potha pa zaka chikwi zimenezi pamene dziko lathu lauchimoli lidzayeretsedwa ndi kuikidwa pansi pa ulamuliro wa Kristu. Chibvumbulutso 20 akutisoneyenza ife kuti zaka chikwi zimenezi zagawidwa mu midzukiro iwiri ya akufa.



Kodi Mulungu adzaukitsa ndani kwa akufa mu mdzukiro woyamba omwe udzachitike ku mayambiriro a zaka chikwizo?

"Wodala ndi woyerwa mtima ali iye amene achita nao pa kuuka koyamba; pa iwowa imfa yochiwiri iribe ulamuliro; komatu adzakhala ansembe a Mulungu ndi a Khristu, nadzacita ufumu pamodzi ndi lye zaka chikwizo." - Chibvumbulutso 20:6.

"Wodala ndi woyerwa" iwo amene anamulandira Yesu ngati Mpulumutsi wawo, akuturuka m'manda mu "Kuuka koyamba". Ngati wolungama "Adzalamulira pamodzi" ndi Khristu munthawi ya zaka chikwiyi, adzayeneradi kuuka kumayambiriro kwake kwa zakazi.

Nanga ndi ati omwe adzauke kwa akufa kachiwiri kumapeto kwake kwa zaka chikwizi?

"Otsala akufa sanakhalango ndi moyo kufikira kudzatha zaka chikwi." - Chibvumbulutso 20:5.

"Otsalawo akufa akutanthauza akufa osalungamawa, chifukwa olungama," wodala ndi woyera" auka kale ku mdzukiro woyamba wa zaka chikwizi.

Choncho nthawi ya zaka chikwiyi ikusonyezedwa bwino ndi kuuka kwa akufa kwa mitundu iwiri: kuuka kwa anthu oyera mtima koyamba, ndi kuuka kwa anthu ochimwa kwa kumapeto kwa zakazi.

2. KUUKITSIDWA PAKUBWERANSO KWA KHRISTU

Kuuka koyambirira, kwa wolungama, kukuchitika pakubweranso kachiwiri kwa Yesu Kristu.



"Pakuti Ambuye adzatsika kumwamba mwini Yekha ndi lipenga la Mulungu, NDIPO AKUFA MWA AMBUYE ADZAYAMBA KUUKA; pamenepe ife okhala ndi moyo, otsalafe, tidzakwatulidwa nao pamodzi m'mitambo, kukakomana ndi Ambuye m'mlengalenga. Ndipo potero tidzakhala ndi Ambuye nthawi zonse." - 1 Atesalonika 4:16, 17.

Podzabwera Yesu kachiwiri kudzikolo lapansi, akudzauksa" akufa mwa Khristu" ndi kuwatenga. Iwo pamodzi ndi olungama amoyo, kupita nawo kumwamba. Popeza wochimwa adzakhala ndi chikangamirire ku uchimo, sangaonekerenso pamaso pa Mulungu, ndipo adzaonongedwa pakudza kwa Khristu (Luka 17:26-30) (Mutha kukawerenganso phunziro lathu la chisanu ndi chitatu lija za zochitika pakubweranso kwa Khristu).

3. SATANA ADZAKHALA MMAUNYOLO A NDENDE KWA ZAKA CHIKWI

Pamene nthawi ya zaka chikwiyi idzayamba, wolungama adzakhala onse atapita kumwamba, ndipo ochimwa onse adzakhala atafa ali m'manda mwawo. Nanga chidzidzachitika ndi chiyani pa dziko lapansi?

"Ndipo ndinaona m'ngelo anatsika kumwamba, nakhala nacho chimfungulo cha phompho, ndi unyolo waukuru m'dzanja lace. Ndipo anagwira chinjoka, njoka yakaleyo, ndiye mdierekezi ndi Satana, nam'manga iye zaka chikwi' namponya ku phompho, natsekapo, nasindikizapo cizindikiro pamwamba pache, kuti asanyengeso amitundu kufikira kudzatha zaka chikwi." - Chibvumbulutso 20:1-3.

Pakubwera kwa Yesu, Satana adzamangidwa nakhala muunyolo mu zaka chikwi. Nanga ndende yake ya Satanayo idzakhala kuti? Ku "phompho", liwu lachihele lotanthauza "Kwakuya kwambiri" kapena "Kopanda malire kupita pansi" Mu Genesis 1-2, m'chiherene cha chipangano chakale, "phompho" likulongosoledwa ngati m'mene dziko lidaliri kusadalengedwe kanthu kali konse. Choncho dziko lapansi ndilo "phompho" la ndende ya Satana komwe Mulungu adzamatsekereko iye.

Mawu a Mulungu akunena zoti Satana adzamangidwa "unyolo waukuru" Kodi umenewu ndi unyolo weni-weni womwe tikuudziwawu? Ayi ukuimira unyolo wa zochitika satana akadakonda kuitiriza kunyenga anthu mu zaka chikwi zimenezi. Koma sangapeze aliyense wolungama chifukwa adzakhala atapita kumwamba. Komanso sangapeze ngakhale munthu mmodzi wochimwa chifukwa adzakhala onse atafa, ali mmunda, kugona mu fumbi la nthaka ya dziko lapansi.



Adzayenda-yenda uku ndi uko m'dziko lopanda kanthu kusowa woti amunamize, ndipo adzaumirizidwa kuganizira za mitima ya anthu yomwe iye adaswa ndi matsoka omwe iye adadza kuwachititsa.

4. OYERA ADZAWERUZA OCHIMWA

Munthawi ya zaka chikwi, idzakhalanso nyengo ya chiweruziro. Koma kumbukirani kuti chiweruziro chirri ndi makhwerero eni eni anayi monga:-

- (i) Chiweruziro cha oyera Yesu asanabwerenso kachiwiri
- (ii) Mphotho ya wolungama pa kubweranso kwachiwiri kwa Yesu
- (iii) Chiweruziro cha wosalungama mu nthawi ya zaka chikwi
- (iv) Mphotho ya satana ndi omutsatira ake kumapeto kwa zaka chikwi. Mutha kubwerezanso phunziro lathu lija la chikhumi ndi chitatu lomwe likulongsola bwino za khwerero loyamba ndi lachiwiri la chiweruziro, ndi (chiweruziro kufufuza ndi mphotho ya oyera mtima).

Panopa tiona khwerero lachitatu ndi lachinayi, kufufuza ndi mphotho la ochimwa. Taona kuti akufa ali woyeru omwe aikitsidwa ndi iwo amoyo oyera akutengedwa onse pamodzi kunka kumwamba pakubweranso kwachiwiri kwa Yesu Kristu. Ali kwawo kumwamba m'nthawi iyi ya zaka chikwi. Kodi adzakhala akuchitako chiyani?

"Kapena kodi simudziwa kuti oyera mtima adzaweruza dziko lapansi?... Kodi simudziwa kuti tidzaweruza angelo?" - 1 Akorinto 6:2-3.

"Ndipo ndinaona mipando ya chifumu, ndipo anakhala pamenepo, ndipo anawapatsa chiweruziro... ndipo anakhala ndi moyo, nachita ufumu pamodzi ndi Khristu zaka chikwi." - Chibvumbulutso 20:4.



M'nthawiyi ya zaka chikwi, oyera adzaonanso mobwereza milandu ya anthu ochimwa ndi angelo akugwa, kuphatikizapo mtsogoleriwawo, satana. Choyeneratu nanga kwa iwo adafera ntchito ya Mulungu, ogonjetsa ndi oima nji mu nkondo yoopsa ya uthenga wabwino, kuti afufuze ndi kumvetsa chiweruzo cha Mulungu pa anthu ochimwa.

Mwachisomo, Mulungu waperekwa mwayi uwu wa kufufuza ntchito zake pa anthu ochimwa, kwa anthu ake oyera. Titha kukhala ndi mafunso ambiri monga ili: "Kodi chifukwa chiyani adzakhali anga siali nafe kuno? Iwo amaoneka munthu wabwino". Tikadzaona m'mabukhu ndi kuweruza akufa; "molingana ndi zomwe adachita zolembedwa m'mabukhuwo"

(1 vesi 12) tidzaona tokha kuti Mulungu ndi wachilungamo ndi aliyense mu zochitika zake zonse pa munthuyu. Tidzaona mmene Mzimu Woyeru udzaperekera mwayi kwa anthu nthawi zosiyana-siyana kuti afikire kwa Mulungu, ndi chilungamo cha chilango chawo chidzaonekera poyeru.

5. SATANA AMASULIDWA PATATHA ZAKA CHIKWI

Kumapeto kwake kwa zaka chikwi, Bukhu Lopatulika likunena kuti:

"Ndipo ndinaona mzinda woyerawo, Yerusalemu watsopano, ulikutsika kumwamba kwa Mulungu, woko nzeka ngati mkwatibwi wokometsedwera mwamuna wace." - Chibvumbulutso 21:2.

Mzinda wozizwitsawu wakhala ngati kwathu kwa zaka chikwi. Ndipo panopa Mzinda woyerawo - pamodzi ndi Khristu ndi opulumutsidwa ake onse ali mkatimo, akutsika kumwamba kudza kudziko lathu lapansi. Kodi satana adzatani pa kutsekeda kwa nthawiyi ya zaka chikwi?

"Ndipo pamene zidzatha zaka chikwi, adzamasulidwa satana m'ndende yace; nadzaturuka kudzasokeretsa a mitundu ali mu ngodya zinai za dziko... kudzawasonkhanitsa achite nkondo, chiwerengero cao ca iwo amene chidzakhala ngati mcenga wa kunyanja. Ndipo anakwera nafalikira m'dziko, nazinga tsasa la oyera mtima ndi mudzi wokondedwawo." - Chibvumbulutso 20:7-9.

Ochimwa akuukitsidwa mu kuuka kwachiwiri pamapeto pa zaka chikwi (vesi 5) Pamene oyera mtima akutsikira ku dziko lapansi ali mu mzinda woyeru ndipo ochimwa akuukitsidwa, satana "adzamasulidwa kwa kanthawi kochepa (vesi 3). Iye adzakhalanso ndi anthu ochimwa awa ngati mtsogoleri wawo ndi oyera monga adani oti achite nawo nkondo. Mosataya nthawi; iye adzayamba kusonkhanitsa ochimwawa ku gulu lalikuru lankhondo. Ndipo adzalamulira iwo kuchita nkondo ndi anthu okhala mu Mzinda Woyerawu. Pamene ochimwa adzidzatenga mbali zavo kuzungulira Yerusalem (vesi 9), adzaona kuopsa kwake kulephera kulowa mumzindawu chifukwa chotaika - tataika tsono kwamuyaya.



6. CHIONETSERO CHA CHIWERUZIRO CHOTSIRIZA

Apa, kwa nthawi yoyamba, anthu a mtundu wake akukumana maso - ndi - maso pamodzi. Yesu akuwatsogolera ana a Mulungu opulumutsidwa omwe ali mkatи mwa Mzindawo. Satana naye akutsogolera chigulu cha anthu ochimwa omwe ali kunja kwa mzindawo. Panthawi yoopsa iyi, Mulungu akupereka chiweruzo chake chomaliza ndipo ochimwa adzalandira zoyenera za mlandu wawo patsikuli.

"Ndipo ndinaona mpando wa chifumu wauku woyera, ndi lye wakukhalapo, amene dziko ndi m'mwamba zinathawa pamaso pace... ndipo akufa anaweruzidwa mwa zolembedwa m'mabuku. Monga mwa ntchito zao." - Chibvumbulutso 20:11, 12.



Pamene ochimwa adzaima pamaso pa chiweruziro cha chilungamo, moyo wao wonse udzatsegukira kuonekera poyeru pamaso pawo, kuchokera m'mabukhu a kumwamba, Yesu, woweruza wachilungamo, adzatambasula mbiri yonse ya zochitika zake pa anthu akugwa, amuna, akazi ndi angelo. Dziko lonse lapansi lidzayang'ana ndi chidwi. Ataima pamaso pa mpando wa Mulungu, Yesu adzapereka umboni wonse womveka wa ntchito yake yakupulumentsa. Adzaulula kuti ndadza kufuna ndi kupulumentsa chotaikacho adadza m'dziko lathu lapansi mwa thupi la umunthu, nakhala moyo wosachimwa pakati pa mavuto ndi mayesero. Adapereka nsembe yokhayo ya pamtanda, natumikira monga wansembe wathu kumwamba. Pamapeto pake, pamene Khristu adzaima

patsogolo, mwachisoni napereka chiweruzo cha iwo okhalabe ochimwa, kukana chisomo chake, ali yense m'dziko adzabvomereza chilungamo ndi kufunika kwake kwa chiweruzo chomalizachi cha Mulungu.

"Pakuti ife tonse tidzaimirira ku mpando wakuweruza wa Mulungu. Pakuti kwalembedwa, pali moyo wanga, ati Ambuye, mabondo onse adzagwadira lne, ndipo malilime onse adzavomereza Mulungu." - Aroma 14:10-11.

"Yesu Khristu... anakhala womvera kufikira imfa ndiyo imfa ya pamtanda!... Mdzina la Yesu bondo lirilonse lipinde, la za m'mwamba ndi za padziko, ndi za pansi pa dziko... Ndi malilime onse avomere kuti Yesu Khristu ali Ambuye, kuchitira ulemu Mulungu Atate." - Afilipi 2:5-11.

Kuyambira nthawi yomwe chimo linayamba, Mdierekei wakhala akunyoza khalidwe lake la Mulungu, kumutsutsa lye kuti ali wopanda chilungamo, koma tsopano mafunso onse adzayankhidwa, ndi zonse zosokonezeka zidzakhala mmalo mwake. Ndipo tsono, munthu aliyense m'dziko adzavomereza kuti Yesu, Mwana wa Nkhosa wa Mulungu, ndi woyenera chikondi ndi chitamando cholinga chonse cha Mulungu ndi ntchito yake tsopano zidzaululika kwathunthu, ndipo khalidwe la Mulungu lidzaima lopanda cholakwa.

Siopulumutsidwa okha ayi, komanso angelo oipawo ndi satana mwini wake adzavomereza kuti njira yake idali yolakwika ndi kuti njira za Mulungu ziri zachilungamo ndi zonna. Onse adzaona kuti choipa ndi kudzikonda zabweretsera iwo kusakondwa ndi kusakhutitsidwa ndipo siziri zoyenera kuitirira.

7. TCHIMO LIKUMANA NDI MAPETO AKE

Ngakhale satana ndi gulu lake lalikulu la anthu ochimwa adzabvomereza kuti njira zake za Mulungu ziri zoyenera, mitima yao sidzasinthika, khalidwe lawo lidzakhalabe chiipire. Ndipo chitatha chiweruzochi, ndi chigamulo chitaperekedwa ochimwawa;

"Anakwera nafalikira m'dziko nazinga tsasa la Oyera mtima ndi mudzi wokondedwawo; ndipo unatsika moto wakumwamba nuwanyeketsa; ndipo mdierekezi wakuwasokeretsa anaponyeda m'nyanja ya moto ndi sulfure... Ndipo imfa ndi Hade zinapereka akufawo anali m'menemo, ndipo imfa ndi Hade zinaponyedwa m'nyanja ya moto. Iyo ndiyo imfa yachiwiri, ndiyo nyanja ya moto ndipo ngati munthu sanapezedwa wolemedewa m'bukhu la moyo, anaponyedwa m'nyanja ya moto." - Chibvumbulutso 20:9-15.

Mu chiweruzo chotsiriza moto wa Mulungu wosatha udzaononga tchimo ndi onse okangamira tchimolo. Satana ndi onse otaikawo adzathedwa ndi "imfa yachiwiri" imfa yosatha yomwe sadzaukanso. Njira yaho yakunkira idzawasiya iwo osayenera kukhala navo pa chisangalalo cheni cheni, naonongedwa naye pamodzi mdierekezi ndi angelo ake. Moto wakumwamba udzayeretseratu dziko lonse lapansi ku tchimo lonse ladziko lonse lapansi; Mulungu adzakhala ndi dziko loyera tsopano, lomwe silingadzaiptsidwenso ndi tchimo kulimbana kwa chabwino ndi choipa, pakati pa Kristu ndi Satana kudzakhala kuthatha tsopano ndipo Khristu adzalamulira tchinga likugwa tsopano pa zochitika zonse za tchimo, ndipo kukudza ulemerero wa dziko latsopano lazotheka zambiri-mbiri.



8. DZIKO LIYERETSEDWA KUKHALA LAT SOPANO

Kuchokera pa kuyeretsa komaliza uku, Mulungu adzalenga dziko lapansi latsopano.

"Ndipo ndinaona m'mwamba mwatsopano ndi dziko latsopano, pakuti m'mwamba moyamba ndi dziko loyamba zidacoka, ndipo kulibenso nyanja... Ndidaona Mzinda woyer, Yerusalem watopano, ulikutsika kumwamba kwa Mulungu.... Chihema ca Mulungu ciri mwa anthu, ndipo adzakhalitsa nao, ndi iwo adzakhala anthu ace, ndi Mulungu Yekha adzakhala nao, Mulungu wao; ndipo adzawapukutira misozi yonse kuichotsa pamaso pao, ndi sipadzakhalanso imfa, ndipo sipadzakhalanso maliro, kapena kulira, kapena chowawitsa; zoyambazo zapita... Taonani, ndichita zonse zikhale zatsopano." - Chibvumbulutso 21:1-5.



Dziko lapansi litabwezeretsedwa ku ubwino wake ndi kukongola kwake kwa pachiyambi, lidzakhala kwavo kwa muyaya kwa anthu opulumutsidwa. Atamasulidwa kukudzikonda, matenda ndi mazunzo, tidzakhala ndi dziko lonse lakuti tilifufuze kulikhala, mwaubale ndipo kwamuyaya tidzakhala pamapazi a Yesu Khristu, kumumvera, kuphunzira

ndi kukonda. (Kuti timve bwino lomwe zambiri za dziko latsopanoli, titha kubwereranso ku phunziro lathu lija lachisanu ndi chinayi).

Kodi inu mukukonzekera kuti mudzakhale kuti pa tsikuli? Kodi mwatsimikiza kukakhala naye Yesu pamodzi mkatì mwa mzindawo? Kapena mudzakhala kunja kwa mzindawo kopanda Khristu namukhala otaika mnyanja?

Ngati mwaika moyo wanu m'manja mwa Yesu Khristu, simuyenera kudzaona inu choopsa chosanenekachi cha kwa iwo akukhala kunja kwa mzindawo omwe azindikira kutaika kwawo kwamuyaya. Palibe kanthu kuti mwakumana ndi zotani m'moyo, mukaika moyo wanu m'manja mwa Yesu tsopano lino, mutha kukhala nawo pa gulu la awo okhala mu mzindawo pamodzi ndi Khristu ndi opulumutsidwa.

Ngati simunatero, perekani mitima yanu tsopano lino kwa Yesu, ndipo lye adzakuzingani inu ndi chikondi ndi chikhululikiro chake. Uwu ndi mwayi wanu, ili ndilo tsiku lanu lachipulumutso lero.

KODI GEHENA NDI CHIYANI NANGA ALI KUTI

Kuombera mfuti mosaganiza kudachitika pamene m' phunzi wina adafika pa sukulu yake napha angapo a anzake mu kalasi. Munthu winanso wokhumudwa amene anachotsedwa ntchito anapita ku ntchito kwake kwa kaleko nakapha mkulu wa pa ntchitopo ndi mfuti. Mayi wina anakankhira galimoto yake m'nyanja atatsekeramo ana ake awiri, nafera m'madzimo.



Pafupifupi mu maiko akulu awiri a m'dziko lapansi, anthu zikwi-zikwi aphedwa pa kuyeretsa kwa m'chiweniweni, chifukwa cha kusemphana mawu kokhala zaka mazanamazana. Amuna, akazi, ana ngakhale makanda aphedwa ndi mfuti, kudulidwa nthulinthuli, kumenyedwa, ndi kugwiriridwa chigololo.

Kulanga uchigawenga woipitsitsawu popereka chilango cha imfa, ngakhale chifukwa chakupha mwankhanzaku, kumatsutsidwa ndi anthu ambiri magulu osagwirizana ndi chilangochi amatsutsa poyeria ndi mokweza mawu, m'kumati chilango choterechi sichaumunthu koma "chachikunja ndi cha usatana." Iwo amafunsa, kodi anthu akuphawa sangathe kupulumutsidwa m'njira iliyonse?

Kodi njira yabwino yeniyeni ya umunthu yoti nkulangira zigawengazi ndiye iti? Mpando wopha ndi magetsi? Ena amaganizira zolasa jakisoni wa mankhwala aululu yemwe amapha munthu wolasidwayo mopanda kumva ululu. Enanso amanena kuti moyo ungachoke mwansanga pongompachika wopalamulayo.

Komatu mwa zonse zokambirana mokhudza mtimazi pa chilango cha imfachi, pali njira imodzi imene aliyense saiganizira. Palibe munthu yemwe amaganizira kuti zigawenga zakupha mwankhanzazi, zimene zimachotsa moyo wa anzawo mopanda chifundo, zimadzilanga zokha pomva kutsutsidwa mu ndingaliro (maganizo) zaho ndi kusautsika mu mtima pofikira kuzunzika mpaka imfa. Palibe, mwachitsanzo, yemwe wapereka ganizo loti zigandangazi zimapsa ndi moto wa mu mtima mwawo pang'onopang'ono mpaka kufa.

Koma a Khristu ambiri oona mtima amaganizira kuti Atate wathu wa Kumwamba adzachita choipa koposa apa. Oipa, iwo amatero, ayenera kuzunzidwa kuti alipire dipo la machimo awo. Kuonjezera apo, iwo amatenga zinthu za mabwalo olangira a Mulungu ngati malo akuzunza kosatha.

Makamakano kodi n'chiyani chimachitika kwa oipa? Kodi mapeto ao akulumikizika bwanji mu chikondi cha Mulungu ndi chilungamo chake? Tiyeni tiyang'ané m'Baibulo kuti tipeze yankho.

1. KUSWEKA MTIMA KOTSIRIZA KWA YESU



Kwa zikwi zisanu ndi chimodzi, Mulungu wakhala ali kudandaulira amuna ndi akazi:

"Uziti nao; Pali Ine; ati Ambuye Yehova, sindikondwera nayo imfa ya woipa, koma kuti woipa aleke njira yake, nakhale ndi moyo." - Ezekiel 33:11.

Mtanda wa Yesu udaonetsera poyeria mmene Mulungu akufunira kupulumutsa mtundu wa anthu wakugwawu. Pamene Yesu analira ndi

mawu akulu pa mtanda, "Atate, muwakhululukire iwo, pakuti sadziwa chimene achita." lye anaonetsera poyeria mtima wake wosweka (Luka 23:34). Atangonena izi, Yesu anaperekayo Wake ndipo, ena amakhulupirira, adafa lye chifukwa cha mtima wosweka (Yohane 19:30, 34).

"Komabe ngakhale ndi chionetsero cha mphamvu choterechi cha chikondi cha Umlungu, anthu ambiri satembenukirabe kwa Yesu. Ndipo monga m'mene uchimo ukulamulirabe m'dziko muno, udzapitirizabe kuchulukitsa chisoni cha mtundu wa anthu. Chotero uchimo uyenera kuonongedwa. Kodi Mulungu akulinganiza motani pofuna kuuthetsa uchimowu?

"Koma tsiku la Ambuye lidzadza ...; m'mene miyamba idzapita ndi chibumo chachikulu, ndi zam'mwamba zidzakanganuka ndi kutentha kwakukulu, ndipo DZIKO NDI NTCHITO ZIRI MOMWEMO ZIDZATENTHEDWA." - 2 Petro 3:10.

Mulungu pomalizira pake ayenera kuyeretsa dziko kulichotsera chivundi chonse ndi kuthetsa uchimo. Iwo amene apitiriza kuumirira uchimo adzaonongedwa ndi moto umenewu wokonzedwera kuononga mdierekezi, angelo ake ndi uchimo kuuchotsa mu dziko lathu lino. Nthawi yowawitsa nanga kwa Yesu pamene akuona moto ukunyeketsa iwo amene lye adawafera pofuna kuwapulumutsa.

2. KODI GEHENA ALI KUTI NANAGA ADZAYAKA LITI?

Motsutsana ndi maganizo ena otchuka, Mulungutu alibe moto umene ulinkuyaka pakali pano kumalo wena otchedwa "Gehena" kumene anthu amapitako akafa. Gehena adzakhala pamene dziko lino liti lidzasandulike nkukhala nyanja yamoto. Mulungu akudikira kudzagumula mulandu wa oipa mu chiweruziro chotsiriza kumapeto a zaka chikwi (Chibvumbulutso 20:9-15).

"Ambuye adziwa kupulumutsa opembedza poyesedwa iwo, ndi kusunga osalungama kufikira tsiku loweruza akalangidwe." - 2 Petro 2:9.

Nthawi yokhayokhayinso lye adzachotsa zonyansa zonse ndi moto woyeretsa.



"Miyamba ndi dziko la masiku ano ndi mau omwewo zaikika kumoto, zosungika kufikira TSIKU LACHIWERUZO ndi chionongeko cha anthu osapembedza." - 2 Petro 3:7.

Mulungu sanalinganizire mpang'ono ponse munthu wina aliyense kudzatsiriza moyo wake m'moto wa gehena. Koma pamene anthu akana kulekana naye satana ndi kuumirirabe kumachimo awo, ayenera potsiriza kulandira zotsatira za kusakha kwavo.

"Pomwepo lye adzanena kwa iwo a ku dzanja lamanzere, chokani kwa Ine otembereredwa inu, ku moto WOKOLEZEDWERA MDIEREKEZI NDI AMITHENGA AKE." - Mateyu 25:41.

Molingana ndi Yesu, ndi liti limene gehenayu adzayambe kuyaka?

"Ndipo monga namsongole asonkhanitsidwa pamodzi, natenthedwa pamoto, motero mudzakhala M'CHIMALIZIRO CHA NTHAWI YA PANSI PAN. Mwana wa munthu adzatuma ANGELO ake, ndipo iwo ADZASONKHANITSA PAMODZI, NDI KUCHOTSA ufumu wake ZOKHUMUDWITSA ZONSE, NDI ANTHU ONSE AKUCHITA KUSAYERUZIKA, NDIPO ADZAWATAYA IWO M'NG'ANJO YA MOTO; kumeneko kudzakhala kulira ndi kukukuta mano." - Mateyu 13:40-42.

Namsongole, yemwe ali anthu ochita zoipa, sakuotchedwa panopa ayi kufikira kumapeto ake a dziko lapansi. Chiweruziro chisanaperekedwe, dziko lonse la m'mwamba ndi lapansi liyenera kutsimikizira kuti Mulungu wachita naye munthu aliyense mwa chilungamo. Monga mudafotokozeredwa tsatanetsatane mu Phunziro 22, mu mkangano waukulu umene ukuchitika pakati pa Khristu ndi satana, satana wakhala akuyesetsa kulitsimikizira dziko lonse lapansi ndi m'mwamba momwe kuti njira ya uchimo ndiyo njira yopambana; Yesu wakhala akuonetsera kuti njira yakumvera ndiyo mfungulo (kiyi) ya moyo wokwanitsidwa.



Pakutha pa zaka chikwi, chionetsero chimenechi chidzatsirizira mu kuweruzidwa kwa satana, angelo ake, ndi oipa. Atatha kutsekulidwa mabukhu omwe adzasonyeze mbali imene munthu aliyense anaichita mu zochitika zazikuluzi, Mulungu adzaponya satana, imfa, ndi manda, pamodzi ndi wina aliyense amene dzina lake "silinapezedwe lolembedwa m'bukhu lamoyo, anaponyedwa m'nyanja ya moto, (Chibumbulutso 20:14, 15). Molingana ndi vesi lotsatiralo, Chibvumbulutso 21:1, Mulungu atatha kuliyeretsa dziko lapansi kuchotsa uchimo kudzera m'moto, lye alenganso "M'mwamba mwatsopano ndi dziko latsopano".

3. KODI GEHENA ADZAYAKA NTHAWI YITALI BWANJI?

Okhulupirira ambiri amalilandira ganizo lakuti moto wa gehena udzayaka kwa tuyaya, kusonyeza chilango chosatha. Tiyeni tione mosamalitsa ndime zimene zimafotokoza mmene Mulungu adzachitire nalo tchimo ndi ochimwa.

"Iye adzabwezera chilango kwa iwo osamdziwa Mulungu, ndi iwo osamvera uthenga Wabwino wa Ambuye Bathu Yesu, amene adzamva chilango, ndicho CHIONONGEKO CHOSATHA chowasiyanitsa ku nkhope ya Ambuye, ndi ku ulemerero wa mphamvu yake." - 2 Atesalonika 1:8, 9.

Chonde onani kuti "chionongeko chosatha" sizifanana ndi "chizunzo chosatha" ai, koma kuti zotsatira zake za chionongeko chimenechi zidzakhala zotsirikiziratu kwa tuyaya. Sichidzabweranso chionongeko china ai. Zochitikazo ndizo imfa yosatha. Petro ananena za tsiku la chiweruziro ndi "chionongeko cha anthu osapembedza" (Petro 3:7).

Molingana ndi Yesu, "moyo ndi thupi" lomwe zidzaonongedwa m'gahena (Mateyu 10:28). Mu chipunxitso chake cha paphiri, Yesu adanena za chipata chopapatiza yomwe ili njira "yakumuka nayo ku moyo" ndi njira yotakata yomwe ili "yakumuka nayo ku kuonongeka" (Mateyu 7:13, 14). Mu Yohane 3:16, Yesu akufotokoza kuti Mulungu "anapatsa Mwana Wake wobadwa yekha." Kuti iwo onse akukhulupirira lye "asatayike, koma akhale nawo moyo wosatha". Yesu akuyerekeza mapeto a zochitika ziwirizi: moyo wosatha kapena kutaika - osati kumangopsabe mpaka tuyaya. Tiyenera tsono kumaliza mwakuti gehena ali ndi mapeto ake otsimikizika: mu imfa ndi m'kuonongeka kwa oipa.

Zolembra zomveka bwino m'malembo opatulika zimatiuza kuti oipa adzaonongedwa.

"Oipa adzadulidwa" (Masalmo 37:28) iwo "adzaonongeka" (2 Petro 2:12) "adzanyeka monga utsi, adzakanganuka" (Masalmo 37:20). Motowo udzawayatsa kuwanyeketsa ndi kuwatsiriza, nasanduka phulusa (Malaki 4:1-3). "Mphotho yake ya uchimo ndi imfa," osati moyo wosatha mu moto wa gehena ayi; "mphatso yaulere ya Mulungu ndiyo moyo wosatha" (Aroma 6:23).

Cholina cha chilango chotsirizachi mu moto wa gehena ndi kuchotsa uchimo pa dziko lonse, osati k usunga kwa nthawi zosatha ayi. Ndi yovuta kwambiri kuganizira kuti Khristu yemwe adakhlulukira iwo amene anamupha lye angakhoze kukhala nthawi zamuyaya akuyang'anira zowawa za iwo olangidwa.



Gehena ndithu ali ndi mapeto ake. Pakutha pa zaka chikwi, Mulungu adzavumbwitsa moto kuchokera ku mwamba ndipo adzachotsa kotheratu mdierekezi, angelo ake ndi wonse oipa amene aumirira ku machimo ao. "Moto" udzatsika "kuchokera kumwamba nuwanyeketsa iwo," (Chibvumbulutso 20:9).

Molingana ndi Yesu, moto umenewu ndi "moto wosazima" (mateyu 3:12). Palibe gulu lina lililonso la zimani moto lomwe lingadzathe kuuzimitsa motowu kufikira utadzachita ntchito yake yonse yakuononga kotheratu.

Mulungu akulonjeza kuti, kuchokera mu moto woyeretsawu, Iye adzalenga, "dziko latsopano," mmene "zovuta zakale zidzaiwalika; ndipo "mau akulira sadzamvekanso mwa iye, pena mau akufuula (Yesaya 65:16-19).


Tsiku lodabwitsa nanga! China chilichonse choyambitsa kusweka mtima kapena kukhumudwitsa chidzachoka. Mulungu adzapoletsa mabala a uchimo ndi kufafaniza zipsera zonse kuzichotsa mu mtima uliwonse, ndipo chimwemwe chathu chidzakhala chodzaza.

4. "NTHAWI ZOSATHA" M'MALEMBA (M'BAIBULO)

Mu Mateyu 25:41 Yesu akunena za "moto wa nthawi zonse wokolezedwera mdierekezi ndi amithenga ake" Kodi mawu akuti "nthawi zonse" apa akupereka ganizo lakuti gehena ndi wamuyaya? Yuda amatipatsa Sodomu ndi Gomora monga "chitsanzo... cha chilango cha moto wosatha." Moonekeratu mizinda imene ija siikuyakabe mpaka lero. Koma motowo unali wosatha muganizo lakuti zimene unachitazo zinali chionongeko chotsimikizika.

Mu 2 Petro 2:6 timawerenganso za moto wosatha. Komano lemba ili limaonetseratu momveka bwino kuti Mulungu "anaisandutsa makala midzi ya Sodomu ndi Gomora anaitsutsa poigwetsa, ataiika. Chitsanzo cha kwa iwo akakhala osapembedza. Osapembedza a mu Sodomu ndi Gomora sali mu chisautsobe mpaka lero ayi; iwo anasandulitsida phulusa kalekale. Komabe moto udawanyeketsawo ndi "wosatha" mu zotsatira zimene udachitazo-chionongeko chotsimikizika. "Kusatha" kutanthauza chilango chotsimikizika ndi chosasinthika, osati kulangika komangopitirirabe.

Popeza buku la Chibvumbulutso limagwiritsa ntchito mawu amaphiphiritso komanso ooneka ngati zinthu zenizeni, zina za ndime zake zamvetsedwa molakwika. Mwa chitsanzo, Chibvumbulutso 14:11 amanena za otaika kuti, "utsi wa kuzunza kwavo ukwera ku nthawi za nthawi." Izitu zimaoneka ngati kuzunzika kopanda mapeto. Koma, mobwerezanso, tiyeni tilole malemba (Baibulo) azimasulire okha.



Eksondo 21:16 akunena za kapolo wobooledwa khutu monga chizindikiro chakuti ayenera kutumikira mbuye wake "kwa tuyaya (kosatha). Apapatu "muyaya" akutanthauza nthawi yonse yomwe kapoloyo akali moyo. Yona, yemwe adakhala m'mimba mwa chinsomba masiku atatu okha ndi usiku wake (Mateyu 12:40) amanena kuti iyeyo adakhala m'menemo "kwa tuyaya" (Yona 2:6). Nzosadabwitsaditu apa chifukwa kukhala mu mdima waukulu mkat i mwa chinsomba kudaoneka ngati tuyaya.

Chotero tiyenera kusamalitsa pofuna kumvetsetsa za mmene ndi nthawi imene Baibulo likugwiritsa ntchito ziphiphiritso kapena mau a chining'a ngati ndakatulo. Utsi wokwera nthawi za nthawi kuchokera ku nyanja ya moto ndi njira yenyeni yomveka bwino pofotokoza kuononga komaliziratu, Chibvumbulutso

21:8 akutiuza poyer a kuti nyanja yotentha ndi moto ndi sulfure ndiyo "imfa yachiwiri". Gehena ali ndi mapeto ake. Oipa anyeketsedwa; iwo aonongedwa.

5. KODI NDI CHIFUKWA CHIYANI KUYENERA KUKHALA GEHENA?

Pachiyambi Mulungu analenga dziko langwi. Koma tchimo linadza ndi kubweretsa mavuto oopsa, chivundi ndi imfa. Inu mutafika ku nyumba kwanu madzulo ena ndikupeza kuti nyumbayo yafwanyulidwa fwanyulidwa ndi kuonongedwa, mungaisiye choncho kwa nthawi zonse? Ndithu ayi. Musesa zinyalala zonse ndi zinyasi zonse, kukonza malo onse, ndi kutaya mipando yonse yothyoledwa mosakaza. Mulungunso naye adzachita chimodzimodzi. Adzakonza zophwasuka ndi zoonongedwa ndi tchimozo kwa nthawi zonse, nkuyeretsa dziko ndi moto n'kuti akonzetsere njira ya dziko langwi momwe mudzakhale anthu opulumutsidwa.



Komano Mulungu akukumana ndi vuto lalikulu popeza tchimo silinangosakaza dziko leni leni lokhalo ayi, komanso linaononga anthu okhala m'dzikomo. Tchimo linasokoneza ubale wathu ndi Mulungu, komanso ndi wina ndi mzake. Umunthu ukupitirirabe kuzunzika ndi vuto la kuzunza ana, kuopsezana pakuphana, kanema wa zaumaliseche, ndi matenda ambiri a khansala yosiyanasiyana ya moyo wauzimu. Chotero Mulungu ayeneradi tsiku lina kuliononga tchimo, chifukwa ilolo likusakaza anthu. Njakata ya Mulungu ili apa: Achotsa bwanji kachilombo koopsa koyambitsa utchimo m'dziko komano osaononga anthu onse omwe ali ndi tchimolo? Yankho lake linali kutenga kachilomboko kakhale m'thupi mwake; kulola kuti khansala ya uchimoyo iwonganje thupi lake pamtanda. Zotsatira:

**"Ngati tivomereza machimo anthu, ali wokhulupirika ndi wolungama lye, kuti atikhululukire machimo anthu, ndi KUTISAMBITSA KUTICHOTSER A CHOSALUNGAMA CHILI CHONSE." - 1
Yohane 1:9.**

Mulungu apa akupereka yankho lake ku vuto la uchimo kwa aliyense kwaulere. Koma chomvetsa chisoni ndi chakuti anthu ena akukangamirabe ku nthenda ya uchimoyi. Ndipo Mulungu sadzawaumiriza iwo kutsata njira Yake ya moyo wosatha. Iwo amene akana yankho lakelo adzanyeketsedwa ndi nthendayi pamapeto pake, cholinga chenicheni cha Gehena ndi ichi:

"Pakuti pamene ndinaitana, inu simunayankhe; pamene ndinanena, simunamve; koma munachita choipa m'maso mwanga, ndi kusankha chimene lne sindinakondwera nacho." - Yesaya 65:12.

Atalekanitsidwa ndi Yesu mwa chisankho chawo, oipa adzafika pozindikira kuti palibenso njira ina yowayenera koma imfa yamuyaya basi.

6. KODI KUTAIKA KUDZAPINDULANJI?

Ngakhale Baibulo siliphunzitsa kuti zotsatira za moto wa Gehena ndi chizunzo chosatha, linatipatsabe masomphenya a zowawa zoopsa zimene adzakumane nazo anthu otaika. Anthu oipa adzausowa moyo wosatha. Choopsatu nanga kuzindikira kuti chimwemwe cha moyo wosatha ndi Mulungu chapulumuka m'manja mwawo, kuti iwo sadzaonanso ukoma ndi kununkhira kwa chiyanjano chokonda ndi changwi cha mibadwo mibadwo.



Pamene Yesu adapachikidwa pamtanda ndi machimo a dziko lapansi kumulekanitsa ndi Atate, ayenera kuti adamva kuwawa kwake kwakutaikiratu kosatha. Monga oipa akamaona chimdimcha phompho lopanda kanthu lili patsogolo pawo, iwo amangoona chionongeko chosatha chokha basi. Pa nthawi

yokhayokhayo, iwo ameonanso m'mene adamkankhira Khristu kutali ndi iwo kawirikawiri pamene lye adadza pafupi ndi zidandaulira za chikondi. Pa mapeto pake, iwo agwa pansi pa maondo awo navomereza chilungamo cha Mulungu ndi chikondi chake (Afilipi 2:10).

Nzosadabwitsa kuti anthu olemba Baibulo amakanikiza pa ife mwachangu kulemera kwake kwa zisankho zathu ndi za zomwe Khristu amanena za lye Mwini.

"Tidandauliranso kuti musalandire chisomo cha Mulungu kwachabe inu, (pakuti anena, m'nyengo yolandiridwa ndinamva iwe, ndipo m'tsiku lachipulumutso ndinakuthandiza, taonani, tsopano ndiyo nyengo yabwino yolandiridwa, taonani, tsopano ndilo tsiku la chipulumutso)" - 2 Akorinto 6:1, 2.

Ndikuganizira kuti palibenso tsoka lina lalikulu loposa la munthu amene wataya nsembe ya mtengo wapatali ya Yesu posankha kutaika. Zisankho zomwe tayang'anana nazo zaonet sedwa poyer a ndi momveka bwino: chionongeko chamuyaya-kulekanitsidwa kwa nthawi zosatha kuchokera ku nkhopre ya Mulungu, kapena ubwenzi wamuyaya ndi Khristu umene udzakhutitsa zolakalaka zathu zakuya. Inu mudzisankhira nokha chiti? bwanji osadzipezera nokha mapeto a moyo wanu mwa Khristu lero?

KODI MUNTHU AKAFA CHIMATSATIRAPO NDI CHIYANI

Timazemba kuyankha funso limene mwana amafunsa kuti. "Kodi kufa ndi chiyani? "Timaganiza kuti ndizovuta kunena kapena kuganiza za munthu amene timamukonda kuti afe. Imfa ndi mdani wodziwika wa munthu kulikonde. Kodi nanga yankho la funso lovutali la imfa ndi chiyani? Kodi munthu akafa pamadzakhalanso moyo wina kwa iye? Kodi tidzathanso kuwaona okondedwa athu amene adafa kale?

1. KUKUMANA NDI IMFA MOPANDA MANTHA

Tonse, nthawi ina yake, mwina pakufa pa mbale kapena bwenzi lathu lapamtimi, timaganizirapo za njala yomwe timamva ngati sitinadye kanthu, komanso kuganizirapo za mmene umasowera bwenzi poona za mapeto a moyo wa munthu.

Mwa mfundu zofunika kwambiri, zodzala ndi maganizo osiyana-siyana, tingaphunzire kuti za choonadi chake cha zomwe zimachitika munthu akafa? Mwa mwayi, mbali ya cholinga cha Yesu padzikolo lapansi inalinso "Kumasula onse iwo amene m'moyo wawo wonse adali mu ukapolo wa mantha a imfa" (Ahebri 2:15). Ndipo mu Baibulo, Yesu akupereka uthenga wolimbikitsa ndi kuyankha momveka bwino mafunso onse athu okhudza imfa ndi moyo ulinkudza.



2. MMENE MULUNGU ADATIPANGIRA IFE

Kuti timvetsetse kuchokera m'Baibulo zoonadi zeni-zeni za imfa, tiyen'i tiyambe kuyambira pachiyambi ndi kuona mmene Mlengi wathu adatipangira ife.

"Ndipo Yehova Mulungu anaumba munthu ndi dothi lapansi (Adamu mu chi Hebre) nauzira mpweya wa moyo m'phuno mwace, munthuyo nakhala wa moyo (Mzimu)." - Genesis 2:7.



Pa chilengedwe Mulungu adampanga Adamu "kuchokera ku fumbu la nthaka" adali ndi uwongo mutu mwace, wokonzekera kuganiza; mwazi mnjira zake, zokonzetsedwera kuti ukuyenda mthupi lonse. Ndipo Mulungu adauzira mphuno mwa munthuyo "mpweya wa moyo" ndipo Adamu adakhala "Munthu wa moyo" (mu chi Hebre, Mzimu wa moyo). Taonetsetsani apa mosamala kuti Baibulo silimunena kuti Adamu adalandira Mzimu ayi; koma likuti "munthu adakhala Mzimu wa moyo."

Pamene Mulungu adauzira mwa Adamu mpweya wa moyo, moyo udayambika kuyenda mwa anthu kuchokera kwa Mulungu. Kulumikizana kwa umodzi wa thupi ndi "mpweya wa moyo" kunapanga Adamu, "munthu wamoyo" choncho tingathe kulemba ndondomeko ya samu yake ya kupanga mwa umunthu motere: "Fumbi la dothi lanthaka" + "Mpweya wamoyo" = "munthu kapena Mzimu wa moyo. "Thupi lopanda moyo + mpweya wa Mulungu = munthu wa moyo" ali yense wa ife amaganiza. Pamene tiri otha kupuma, tidzakhala amoyo ndithu, mzimu wa moyo.

3. CHIMACHITIKA NDI CHIYANI MUNTHU AKAFA?

Pakufa, zimachitika ndi zosiyana ndi zija, zapachilengedwe za pa Genesis 2:7 ndizo zimachitika: "**pfumbi ndi kubwerera pansi pomwe tinali kale, mzimu ndi kubwerera kwa Mulungu amene anaupereka.**" - Mlaliki 12:7.

Baibulo nthawi zambiri limagwiritsa ntchito mawu a chi Hebri pa liwu la "mpweya" ndi "Mzimu" mosinthana - sinthana pamene anthu afa, matupi awo amasandulika "fumbi" ndipo "mzimu" (mpweya wa moyo) umabwerera kwa Mulungu, kumene udachokera. Nanga kodi chinachitika ku munthu (mzimu wopangidwa) ndi chiyan?

"Pali Ine, ati Ambuye... Miyoyo yonse ndi yanga, monga moyo wa Atate momwenso moyo wa mwana...moyo wochimwawo ndiwo udzafa." - Ezekiel 18:3-4.

Moyo umafa! Panopa siuli wosafa ayi - utha kuonongeka. Samu ya kapangidwe ija yochokera pa Genesis 2:27, pamene Mulungu adatipanga ife, imadzitembenuzanso yokha pamene tifa

"fumbi la kunthaka" - **"mpweya wa moyo = "mzimu wakufa"**
"thupi lopanda moyo" - **"phweya wa Mulungu"** = **Munthu wakufa**

Imfa ndi kutha kwa moyo. Thupi limaphwasuka kusandulika dothi, ndipo mpweya , kapena mzimu umabwerera kwa Mulungu. Ife ndife anthu chifukwa cha moyo, koma timakhala mitembo tikafa. Choncho akufa saganiza ayi, pamene Mulungu watenganso mpweya wake wa moyo womwe adaupereka, miyoyo yathu imatha, timafa. Koma m'mene tionere kutsogoloku, mu phunziroli, mwa Khristu tiri ndi chiyembekezo

4. KODI MUNTHU WAKUFA AMADZIWA ZINTHU ZOTANI?

Tikafa, uwongo umaphwasuka, suthanso kudziwa kapena kukumbukira chirichonse. Zonse zochitika mwa munthu zimaima munthuyo akafa.

"Chikondi cao ndi udano wao ndi dumbo lao lomwe zatha tsopano..." - Mlaliki 9:6.

Akufa sadziwa kanthu, choncho sathanso kuzindikira za zochitika ziri zonse. Iwo ali olekanitsidwa kwathunthu ndi a moyo.

"Pakuti amoyo adziwa kuti adzafa; koma akufa sadziwa kanthu bi" - Mlaliki 9:5.

Imfa iri ngati tulo topanda maloto - ndiponso, Baibulo litchula imfa monga "tulo" kwa nthawi makumi asanu mphambu zinayi. Yesu adaphunzitsa kuti imfa ili ngati tulo. Adati lye kwa ophunzira ake.



"Lazaro bwenzi lathu ali mtulo; koma ndimuka kukamuukitsa iye tulo tace, chifukwa chace akuphunzira ace anati kwa lye, Ambuye, ngati ali m'tulo adzacira. Koma Yesu adanena za imfa yache, koma iwowa anayesa kuti ananena za mpumulo wa tulo. Pamenepe Yesu anati kwa iwo momveka, "Lazaro wamwalira." - Yohane 11:11-14.

Lazaro adafa nakhala masiku anayi Yesu asadatulukile koma pamene Yesu adapita kumanda kwake kwa Lazaro adatsimikizira poonetsa kuti ndi kwa pafupi kwa Mulungu kuukitsa akufa, monga momwenso ziri ndi ife kudzutsa nzathu amene ali mtulo. Ndichopatsa chitonthozo kudziwa kuti abale athu okondeka omwe tidalekana nawo mu imfa ali "mtulo" kupuma mwa mtendere mwa Yesu. Njira ya imfa imene ifenso tidzadutsanso tsiku lina, iri ngati tulo tafulu takachetechete.

5. KODI MULUNGU AMAWAIWALA OGONA MU IMFA?

Kufa simathero a mbiri pa mmunda wa manda, Yesu adati kwa Marita, mchemwali wake wa Lazaro;

"Ine Ndine Kuuka ndi Moyo: wokhulupirira Ine angakhale amwalira, adzakhala ndi moyo." - Yohane 11:25.

Iwo amene afa "Mwa Kristu" amakhala ali m'tulo mmunda mwawo - koma tsogolo lawo limankhala lowala. Yemwe amatha kuwerenga ngakhalle tsitsi lapamutu pathu natigwira ife kutinyamula mmanja mwake sadzatiiwalanso ife.

Titha kubwerera kunthaka titafa, koma mbiri yathu imakhalabe yoonekera poyer a Mulungu ndipo pamene Yesu adzabwera, adzaukitsa akufa ali oyera mitima onse ku tulo tawo, monga mmene adachitira ndi Lazaro.

"Koma sitifuna , abale kuti mukhale osadziwa za iwo akugona, kuti mungalire monganso otsalawo, amene alibe Chiyembekezo... Pakuti Ambuye adzatsika kumwamba mwini Yekha ndi mpfuu, ndi mau a mngelo wamkuru, ndi lipenga la Mulungu; ndipo akufa mwa Ambuye adzayamba kuuka; pamene po ife okhala ndi moyo, otsalafe, tidzakwatulidwa nao pamodzi m'mitambo, kukakomana ndi Ambuye mumlengalenga, ndipo potero tidzakhala ndi Ambuye nthawi zonse. Chomweco, tonthozanani ndi mau awa." - 1 Atesalonika 4:13, 16-18.

Pa tsiku la m'dzukiro, njira ya imfa idzakhala ngati kupuma kwakamphindi. Akufa sakuona kudutsa kwa nthawi. Iwo amene alandira Khristu monga Mpulumutsi wawo, adzaukitsidwa ku tulo tawo ndi liu la Ambuye lozizizwitsa lobwera ku dziko lapansi. Chiyembekezo cha kuuka kwa akufa chiri ndi mnzake? Chiyembekezero cha kukhala kumwamba komwe Mulungu "adzapukuta misozi iri yonse m'maso a anthu. Sikudzakhalanso imfa, kulira kapena maliro ndi zowawa ziri zonse.

(Chubvumbulutso 21:4). Onse okonda Mulungu sayenera kuopa imfa, kupitirira imfa pali moyo wa muyaya wokwanira ndi Mulungu. Yesu wagwiriza "Mfungulo wa imfa" (Chibvumbulutso 1:18 popanda Khristu, imfa ikadakhala njira ya chimaliziro cha zonse, koma ndi Khristu, pali tsogolo la chiyembekezo chodala chowala.

6. KODI NDIFE OSAFA TSOPANO LINO?

Pamene Mulungu adalenga Adamu ndi Hava, adawalenga iwo kuti adzafa, koma akadakhalabe omvera Mulungu sakadafa, koma atachimwa, adataya ufulu wawo wokhala ndi moyo.

Posamvera Mulungu adasandulika kukhala oti atha kufa. Tchimo lawo lidakhudza mtundu wonse wa anthu, ndi pakuti ali yense adachimwa, tiri ife oti titha kufa, (Aroma 5:12). Ndipo Baibulo silikufotokoza pali ponse kuti munthu amadziwanso kanthu kali konse akafa ayi.



Palibe pomwe Baibulo lidafotokozapo kuti mzimu tsopano uli woti sungafe. Mawu onse a chi Hebri ndi chi Herene onena za "Mzimu" kapena "Mpweya wa moyo" akunenedwa mwa nthawi chikwi, mazana asanu ndi awiri. Koma palibe ngakhale pamodzi pomwe adanena kuti izi sizidzafa. Panopa Mulungu Yekha ndiye ali wosafa.



"Mulungu...amene lye yekha ali nao moyo wosatha." - 1 Timoteo 6:15, 16.

Mawu a Mulungu akulongosola momveka bwino kuti anthu a moyo uno ndi akufa: adzayenera kufa, koma Yesu akadzabweranso, machitidwe athu adzasinthika kwakukuru **"Taonani, ndi kuuzani chinsinsi; sitidzagona tonse, koma tonse tidzasandulika, m'kamphindi, m'kuthwanima kwa diso, pa Lipenga**

**Iotsiriza, pakuti lipenga lidzalira, ndipo akufa adzauksidwa osabvunda, ndipo ife tidzasandulika.
Pakuti chobvunda ichi ciyenera kubvala chisabvundi, ndi cha imfa ichi kubvala chosafa." - 1
Akorinto 15:51-53.**

Monga anthu, sitiri ife osafa panopa; koma chilimbikitso cha Ukhristu ndicho chakuti tidzasandulika osafa pamene Yesu adzabwerenso kachiwiri. Panganoli liri loona ndipo lidatsimikiziridwa kuona kwake pamene Yesu adang'amba manda ake kuwatsegula, lye naturukamo wamoyo ndipo; "**anatha imfa ndipo... naonetsera poyer moyo ndi cosavunda mwa uthenga wabwino**" - 2 Timoteo 1:10.

Kuona kwa Mulungu pa mapeto a munthu kuli komveka bwino lomwe imfa yamuyaya kwa iwo okana Khristu ndi kukamatira ku machimo; kapena kusafa monga mphatso pamene Yesu adzabwerere iwo amene amulandira lye monga Ambuye ndi Mpulumutsi wawo.

7. KUKUMANA NDI IMFA YA OKONDEDWA ATHU

Mantha amene timavutika nawo nthawi zambiri ndiwo a imfa ndipo amafika pachimake pamene wokondedwa wathu amwalira. Kusoweka kwathu kwa kutaika kwake kumakhala kowawitsa. Yankho lenileni la izi ndi kulimbikitsa ndi pa zoti timuona Khristu wotonthozayo, kumbukirani kuti wokondedwa wanuyo ali m'tulo, ndipo ngati agona mwa Khristu adzauksidwa mu "kuuka kwa moyo" pamene Yesu adzabwera.



Mulungu akukonza kukumana ndi kugwirananso kozizwitsa ana adzabwezeredwa kwa makolo awo. Amuna nadzabwezeredwa kwa akazi awo nakumbatirana m'dzanja la wina ndi mnzake. Kulekanitsidwa kwa nkhanza kwa moyo uno kudzatha. "Imfa yamezedwa mu chigonjetso" (1 Akorinto 15:54). Ena amaona ngati angathe kulumikizana ndi okondedwa awo omwe adalekana nawo kupyolera mu za mizimu (ziwanda) kapena matsenga. Koma Baibulo likufotokoza mwa chindunji kutichenjeza ife kuti tisalestse vuto la imfa mwa njira imeneyi.

"Ndipo pamene iwo adzati kwa iwe, funa kwa olaula ndi obwebweta, amene alira pyepye, nang'ung'udza; kodi anthu sadzafuna kwa Mulungu wao? Chifukwa ca moyo, kodi adzafuna kwa akufa?" - Yesaya 8:19.

Nzoonadi, chifukwa chiyani? Baibulo likufotokoza momveka bwino kuti akufa sadziwa kanthu. Choncho yankho la zopweteka zonse zokhuzana ndi kulekanitsidwa kwathu ndi okondedwa athu ndi chitonthozo chochha cha kwa Kristu basi. Kukhala ndi nthawi yolumikizana ndi Kristu ndiyo njira yokhayo yabwino kukula m'mavuto. Kumbukirani nthawi zonse, atafa okhulupirira Khristu adzagona ndi kudzidzimuka kwa kutulo lawo kudzakhala mfuu ya kubweranso kwachiwiri kwa Khristu kudzawauksita iwo ku imfa.

8. KUKUMANA NDI IMFA MOPANDA MANTHA

Imfa inatichotsera pafupifupi chiru chonse. Koma chinthu chimodzi chomwe siingatenge ndicho Khristu; ndipo Khristu atha kubwezeretsa zonse zomwe imfa ingatenge kwa ife imfa sidzalamulira nthawi zonse padziko lapansi, mdierekezi, woipa, imfa ndi manda zidzathera mu "ng'anjo ya moto" imene iri "imfa yachiwiri" (Chibvumbulutso 20:14).

Dotolo wina wamphamu wotchedwa Dr James Simpson yemwe adapanga mankhwala othetsa ululu, adakhuzidwa ndi chisoni chachikulu ndi imfa ya mwana wake woyamba. adalira kwakukuru monga momwe kholo liri lonse lichitira koma adapeza njira ya ku chiyembekezo. Ndipo pa munda wa manda a mwana wakeyu adamangapo chizindikiro nalembapo mau awa omwe Yesu adanena okhuzana ndi kuuka kwake kwa akufa; "Ngakhale ziri chonchi. Ndiri ndi moyo."

Izi zikunena zonse, matsoka a munthu ngoonetsa ngati afufuta miyamba, nthawi zina; komabe ngakhale zitero, Yesu ali wa moyo! Mitima yathu itha kusweka; komabe, Yesu aliwamoyo! Mwa Khristu, tiri ndi chiyembekezo cha moyo ngakhale titafa. Iye ali "kuuka ndi moyo" (Yohane 11:25), ndipo akulonjeza "Chifukwa chakuti ndiri wa moyo, inunso muli a moyo" (Yohane 14:19). Khristu ndiye chiyembekezo chathu chokha cha moyo ngakhale timwalira. Ndipo akadzabweranso adzatipanga ife osafa. Sitidzakhalanso m'chigwa cha mthunzi wa imfa, chifukwa tidzakhala tiri ndi moyo wosatha. Kodi inu mwapeza chiyembekezochi choti tidzikhala nacho munthawi zathu zowawitsa? Ngati simunamulandire Yesu monga Ambuye ndi Mpulumutsi wanu, simungatero tsopano lino?

KODI NDINGAPEZE MPINGO WA MULUNGU LERO

Mulungu, nthawi zambiri, wapereka uthenga wapadera kuti akathetse zosowa zosiyana-siyana za mibadwo yosiyanayi: Uthenga wothandiza Adamu ndi Hava, pamene tchimo lidaononga dziko lawo, uthenga ku dziko lapansi chisanadze chigumula, uthenga kwa ana a Israyeli. Pamene Asiliya ndi a ku Babulo adawaopseza iwo Yesu adabwera ndi uthenga wapadera wa mbadwo wake, ndi Mulungu wapereka uthenga wa padera wa nthawi yathu ino. Mutu wakhumi ndi chiwiri ndi wa khumi ndi chinayi wa Chibvumbulutso ukunena mwachidule uthenga wa Mulungu wapadera kwa ife lero. Mu phunziro lotsogolera ndi lina lotsatiralo, tiona za uthenga umenewu.



1. MPINGO WOKHAZIKITSIDWA NDI YESU

Moyo ndi ziphunzitso za Yesu zidakhazikitsa umodzi wa chikhulupiriro ndi kupembedzera pamodzi mu mpingo wa atumwi womwe iye adayambitsa. Atumwiwo adayambitsa ubale ndi Khristu, weni-weni. Pauloakuuyerekeza ubalewo, pouwona, ndi chiyanjano cha ukwati.

"Pakuti ndinapalitsana ubwenzi mwamuna modzi, kuti ndikalangiza inu ngati namwali woyeria mtima mwa Kristu." - 2 Akorinto 11:2.

Monga mwa kulongosola kwa Paulo, mpingo wa Mulungu uli ngati namwali wangwiro, woyeria, mkwatibwi wa Khristu, choimirira cha mpingo wake wokondedwa wa Khristu. Mu chipangano chakale, chizindikiro chomwechonso chikugwiritsidwa ntchito kusonyeza za Israyeli, mtundu wa anthu wosankhidwa wa Mulungu. Mulungu anati kwa Israyelo "monga mkwatibwi udandikonda Ine" (Yeremiya 2:2) "ndiri mwamuna wako" (Yeremiya 3:14). Bukhu la Chibvumbulutso likunenanso za mpingo monga ngati mkazi.

"Ndipo chizindikiro chachikuru chinaoneka m'mwamba; mkazi wavekedwa duwa, ndi mwezi kumapazi ace, ndi pamutu pace korona wa nyenyezi khumi ndi ziwiri." - Chibvumbulutso 12:1.



(1) Mkaziyu wavekedwa "ndi duwa." Izi zikutiganiziritsa mpingo wowala monga duwa chifukwa chovala Khristu ndi ulemerero wake. Yesu, "kuwala kwa dziko lapansi" (Yohane 8:12), akuwalira mwa wokhulupira aliyense mu mpingo wake, ndi wonse amakhala "kuwala kwa pa dziko lapansi" (Mateyu 5:14).

(2) Mkaziyu wavekedwanso "mwezi kumapazi kwake." Mwezi umasoneyezera kuwala kotengedwa kuchokera kwina kwake, kwa uthenga mu nsembe ndi ziphunzitso za anthu ake a Mulungu mu nthawi ya chipangano chakale mwezi wokhala "pamapazi pake" ukuganiziritsa za kuwala kotengedwa kwina kwa uthenga wabwino kumene kuimirira utumiki wa Yesu Khristu.

(3) Mkaziyu alinso ndi "korona wa nyenyezi khumi ndi ziwiri pamutu pake." Nyenyezi zimaimira mwachinduji atumwi khumi ndi awiri, amuna omvera omwe umboni wawo wapa Yesu umawala kwakukuru mpaka lero. Momveka bwino, maonekedwe a mkaziyo

akulongosoledwa ndiYohane a kusonyezera kuti Yohane uyu adali ndi maganizo a kusinthika kuchokera ku kukhala anthu a Mulungu, Israyeli, wa mu chipangano chakale, kunka ku mpingo wa Khristu wa chipangano chatsopano umene Yesu Khristu adaukhazikitsa. Dzuwa, mwezi, ndi nyenyezi zikutsimikizira uthenga
wa kupatsa moyo wa mpingo wa Mulungu mu utumiki wakugawana uthenga
wabwino.

2. KUGONJETSEDWA KWA SATANA

Kudza kwa mkazi kukubweretsa zochitika zambiri:

"Ndipo anali ndi pakati; ndipoapfuula ali mkubala, ndi kumva zowawa za kubala. Ndipo chioneka chizindikiro cina m'mwamba, taonani chinjoka, choifiira, chachikuru, cakukhala nayo mitu isanu ndi iwiri, ndi nyanga khumi, ndi pamutu pace nduwira zachifumu zisanu ndi ziwiri. Ndipo mchira wace uguza limodzi la magawo atatu a nyenyezi za m'mwamba, nuziponya padziko. Ndipo chinjoka chinaimirira pamaso pa mkazi akuti abale, kuti, akabala, icho chikalikwira mwana wace. Ndipo anabala mwana wamwamuna, amene adzaweruza mitundu yonse ndi ndodo yachtsulo; ndipo anakwatulidwa mwana wace amuke kwa Mulungu, ndi kumpando wachifumu wace." - Chibvumbulutso 12:2-5.

Anthu atatu ofunikira ndiwo ali muzochitikazi:

- (i) Mkazi; yemwe waonetsedwa kale ngati mpingo wa Mulungu
- (ii) Mwana wamwamuna, wobadwa mwa mkaziyu "watengedwe kuptitsidwa kwa Mulungu ndi kumpando wake wachifumu" ndipo tsiku lina "adzalamulira mitundu yonse" Yesu ndiye mwana yekhayo adabadwa mu dziko lino lapansi, natengedwa kunka ku mpando wachifumu wa Mulungu ndipo tsiku lina adzalamulira mitundu yonse.
- (iii) Chinjoka chaimira mdirekezi, kapena satana, **"ndipo munali nkhondo m'mwamba Mikayeli ndi angelo ace akucita nkhondo ndi chinjoka, chinjokanso ndi angelo ace chinacita nkhondo, ndipo sichinalakika, ndipo sanapezekanso malo ao m'mwamba. Ndipo chinaponyedwa pansi chinjoka chachikuru, njoka yokalamba yo, iye wochedwa mdierekezi ndi satana, wonyenga wa dziko lonse, chinaponye-dwa pansi ku dziko, ndi angelo ace anaponyedwa naye pamodzi."** - Chibvumbulutso 12:7-9.



Izi zikuonekera bwino pamene timvetsetsa zizindikiro ndi matanthauzo ake, pamene mdierekeze ndi angelo ake "adasiya malo ao m'mwamba" adaponyedwa kudziko lapansi pamene Yesu anabadwira m'dziklo lino lapansi, mdierekezi adafuna kuti amuphe lye, mwana wa mwamunayo. Atangobadwa kumene, koma adalephera, " ndipo Yesu adakwatulidwa" kupita kumpando wake wachifumu wa Mulungu. Ndipo tsopano satana ananka namaononga mpingo wa Khristu womwe Khristuyo adaukhazikitsa. Mtumwi Yohane, yemwe adalemba Chibvumbulutso, adaona za nkhondo yaikuru pakati pa Khristu ndi satana ikubwera ku dziko lapansi. Pamene nkhondoyi ikufika pachimake peni-peni pa kufa kwa Khristu Yesu kwa kupachikidwa, Yohane akumva mpfuu wa mawu ochokera kumwamba.

"Ndipo ndinamva mawu akuru m'mwamba, nanena, Tsopano cafika chipulumutso, ndi mphamvu, ndi ufumu wa Mulungu wathu ndi ulamuliro wa Khristu wace; pakuti wagwetsedwa wonenera wa abale athu, wa kuwanenera pamaso pa Mulungu wathu usana ndi usiku." - Chibvumbulutso 12:10.

Yesu adagonjetsa satana pa mtanda paja moonekeratu. Ndipo adatsimikizira kukhalako kwake kwa chikonzetsero cha "Chipulumutso" ndi kupereka "mphamvu" zakukanira machenjerero a satana kuwagonjetsa; "Ufumu wa Mulungu" udakhala wotetezedwa, ndipo "Udindo wa Mpulumutsiyo" kukhala wa nsembe wathu wamkuru ndi Mfumu yathu udatsimikiziridwa.

"Panopa tsono chafika chipulumutso" kuonetsera kuti mbiri yonse yakwaniritsidwa. Kubadwa kwa Yesu Mpulumutsi wadziko lapansi kwachitika (vesi 5) Ngakhale satana adayesera kuopseza, koma Yesu adakhala moyo wosachimwa, nafa ndi kuuka kugonjetsa tchimo ndi imfa (vesi 10) satana wagonjetsedwa kwa tuyaya (vesi 7-9) Mtanda wakuzidwa m'mphamvu zake zonse.

Kulemekeza koti "Tsopano yafika nthawi ya chipulumutso" sikosangalatsa Yohane yekha ayi, komanso dziko lonse lapansi.



"Chifukwa cace, kondwerani, miyamba inu, ndi Inu akukhala momwemo. Tsoka mtunda ndi nyanja, chifukwa mdierekezi watsikira kwa inu, wokhala nao udani waukuru, podziwa kuti kamtsalira kanthawi." - Chibvumbulutso 12:12.

M'mwamba monse mukondwerera chigonjetso cha Yesu Kristu adaononga zonse zomwe satana amati ndi zake kumwamba, ndipo satana wogonjetsedwayo adalibenzo kanthu kake ngakhale m'dziko lathu lino lapansi.

3. MPINGO WA KHRISTU ULI PAMKANGANO NDI SATANA

Yesu asadakwere kunka kumwamba, adakhazikitsa mpingo wake (chizindikiro cha mkazi). Imfa yake ya pa mtanda idapereka mphamvu zogonjetsera satana ku mpingo wake.

Ndipo iwo (Akhristu) anamlaka lye chifukwa ca mwazi wa Mwana wa Nkhosa, ndi chifukwa ca mau a umboni wao kungakhale kufikira imfa." - Chibvumbulutso 12:11.

Kristu panopa akutha kupereka mphamvu zake, yomwe iri mphatso ya chigonjetso chake, kwa mpingo wake, Yesu mogonjetsa satana adaonekera pa mtanda paja ndipo akupitirira kuonekerabe ndi chigonjetsochi kupyolera mu Mpingo wake. Pali zizindikiro zoonetsera zitatu za mpingo wogonjetsa mu nthawi yakalelo ya Chikhristu:

(i) "Adamlaka lye (satana) ndi mwazi wa Mwanawankhosa" Yesu adatengedwa kupita kumpando wa chifumu wa Mulungu kuti mwazi wake ukapangike kukhala ndi chikoka mu miyoyo ya omutsatira ake. lye angathe kufufuta machimo athu onse, ndi kutipulumutsa mu mwazi wake wokhetsedwa (Yohane 1:7), ndikutipatsa ife mphamvu za kukhala moyo wabwino wachikristu tsiku ndi tsiku.



(ii) "Iwo sadakonde miyoyo yaho kuti akaope imfa" "Mwazi wa mwanawankhosa" udawapanga iwo kulola kufa chifukwa cha Khristu, ndipo iwo "sadaope imfa" Mulungu adazunzika kwambiri, ndipo awa ofera dzina la Khristu adaloleranso kuzunzika ndi kufa. Ngakhale ena adapanda nsembe yoyenerera. Nthano ikunenedwa ya Mayi wina wachikristu yemwe adaponyedwa mu dzenje la mikango mu nthawi ya ulamuliro wa chi Roma chifukwa chakuti iye adatsimikizira kukhala ndi kuchita za Yesu osati za dziko. Mwana wake wamkazi wang'ono, mmalo moti achite mantha ndi kubwera m'mbujo, adamva mumtima

mwake chikakamizo cha kudzipereka. Pamene mikango inalimbana ndi a Mayi ake, iye adaima kuonerera akulira nati. "Inenso ndine mkhristu" Akulu akulu achi Roma adam'manga iye namuponyanso ku zilombo zolusazo.



(iii) "Iwo adamugonjetsa iye (satana)...ndi mau a maumboni awo" osati mawu okha, koma liwu la umboni wawo; umboni wa moyo wawo, kukhala moyo wa umboni ku mphamvu ya Yesu ndi uthenga wake. M'nthawi ya mdima woopsa wa nthawi ya chi Khristu, asilikari a gulu lankhondo - kuchokera mu mpingo likutsogolera iwo akuteteza mpingo wake wa Mulungu potsutsana ndi dziko. Iwowa adagonjetsa mdierekezi ndi choipa chake chonse pa iwo, pongochitira umboni ndi ntchito za miyoyo yawo.

Pa Chibvumulutso 12:11 akuonetsera mpingo wodzala ndi anthu ogonjetsa; atumwi, ofera ntchito ya Khristu, osungitsa choonadi, ndi ena onse okhulupirira, chifundo chawo, kukhulupirika kwavo, kulimba mtima kwavo ndi chigonjetso chawo chachita bingu mu nthawi zonse za dziko lapansi.

Popeza kuti satana analephura kuononga Yesu pamene anakhala pa dziko lapansi, panopa tsopano akufunitsitsa kuononga a Khristu amene ali mu mpingo wake.

"Ndipo pamene chinjoka chinaona kuti chinaponyedwa pansi kudziko, chinazunza mkazi amene adabala mwana wa mwamuna. Ndipo anapatsa mkazi mapiko awiri a chiomba nkhangha chachikuru, kuti akaulukire ku chipululu, ku mbuto yace, kumene adyetsedwako nthawi, ndi nthawi, ndi nusu la nthawi, osapenya nkhopre ya njoka. Ndipo inalabvulira m'kamwa mwace, potsata mkazi, madzi ngati m'tsinje, kuti akakokoloredwe mkazi nawo. Ndipo dziko linathandiza mkaziyo, ndi dziko linatsegula m'kamwa mwace, nilimeza madzi a mtsinje amene chinjoka chinalabvula m'kamwa mwace." - Chibvumbulutso 12:13-16.

Monga m'mene zinaloseredwa, mu nthawi ya mdima waukuru wa nyengo ya chi Khristu, satana adatuma "mtsinje" wa chizunzo chakupha "kuti uyeretse kusesa" mpingo "ndi madzi othamanga" satana akufuna kuononga chikoka cha Mulungu pochotsa mpingo wake ndi pogwiritsa nzeru za chining'a mmene angathere za kuipa kwake pochita izi. Njoka ikuimira satana kuyambirira, komanso kumbukirani kuti satana amagwiritsa ntchito mabungwe a anthu mu ntchito yake monga njoka kuti agonjetse anthu a Mulungu. Adagwiritsa ntchito mfumu ya chi Roma, Herode kuyesera kupha Yesu Khristu mwanayo atangobadwa kumene. Adagwiritsa ntchito adani a Yesu opembedza a kaduka kuzunza ndi kupachika Mpulumutsi; nafika pachimake popachikitsa Yesu pa mtanda. Koma chigonjetso cheni-cheni cha satana chidasandulika chigonjetso chachikuru cha Kristu.



Pokwiya ndi kugonjetsedwa kwake pamtanda, satana wautembenzira mkwiyo wake ku mpingo umene Yesu adakhazikitsa. Muzaka makumi makumi zotsatira atafa Yesu mopachikidwa, zikwi za anthu adaphedwa mu ulamuliro wa chi Roma, m'mizinda, m'zipululu ndi m'malo ena onse.

Poyamba, maukulu a dziko adalimbikitsa chizunzo ndinenachi. Koma atafa atumwi, kusintha kudabwera mu mpingo. Mu zaka za mazana awiri; atatu ndi anayi; anthu ambiri adayamba kukweza choonadi chomwe Khristu ndi atumwi ake adachiphunzitsa. Atsogoleri ena otsutsana ndi izi adayambapo kupha okhulupirira omwe adaima nganganga pa chiyero cha m'chipangano cha tsopano ndi zikhulupiriro zake.

Aphunzi amayerekezera kuti pafupifupi zikwi zikwi makumi asanu za anthu okhulupirira adaonongedwa poyesera kuumiriza mpingo ndi kuuononga, mdierekezi adatuma "mtsinje" wa chizunzo kuti usese mpingo ndi madzi othamanga mwa liwiyo, kuuchotsa:..."koma dziko lapansi lidathandiza mkaziyo,.... Pomeza mtsinjewo" wa masautso ndi umboni wabodza.

Munthawi ya mkatikati mwa chisautsochi, mpingo woona udachokamo mu utsogoleri wa mipingo yonama, naubisala mu "Chipululu, ku malo okonzetsedwa iwo ndi Mulungu, kumene ukasamalidwa bwino kwa masiku chikwi, mazana awiri ndi mphambu makumi asanu ndi limodzi (1260 days) (vesi 6) ulosi uwu udakwaniritsidwa m'zaka zimenezi za chikwi, mazana awiri ndi makumi asanu ndi limodzi za chisautso kuyambira m'chaka cha 1798 (tsiku loimira chaka mu zizindikiro wa ulosi wa Baibulo. Onani pa (Ezekiel 4:6).

Munthawi ya zaka zamdimayi, a Khristu okhulupirika adapeza mpumulo wawo pali ponse pamene iwo adakhala, monga ku chigwa cha Waldens ku zambwe kwa dziko la Italy, ndi kum'mawa kwa dziko la France, komanso mu mpingo wa ku Celt wa ku zilumba za ku Britain.

4. MPINGO WA MULUNGU M'MASIKU ATHU ANO

Apa tikudza ku nthawi yathu ino- ku mpingo woona wa Mulungu kuyambira m'chaka cha 1798. Monga zingayembekezedwe, mdierekezi adakalibe wokwiya ndi anthu ake a Mulungu, nkondo yosaonekerayo ikupitirirabe. Ndipotu satana, cholinga chake chiru pakugonjetsa mpingo Khristu asanabwere.

"Ndipo chinjoka chinakwiya ndi mkazi, nicinacoka kunka kucita nkondo ndi otsala a mbeu yace, amene asunga malamulo a Mulungu, nakhala nao umboni wa Yesu." - Chibvumulutso 12:17.

Ulosiwu ukunena za nthawi ya masiku athu ano. Satana wakwiya; akuchita nkondo pa "Otsala" a mbewu ya mkaziyo" - anthu ake a Mulungu a lero. Onani mosamala zizindikiro za anthu ake amenewa:



- (i) Anthu okhulupirira a masiku otsirizawa "amamatira ku umboni wa Yesu" kumamatira mokhulupirika ku ziphunzitso zoyenera za mawu a Mulungu, kwapangitsa iwowa kuchitira umboni za Yesu pakukhala moyo wodabwitsa kwambiri.
- (ii) Anthu okhulupirira a masiku otsiriza ndi anthu a ulosi. Kulandira "umboni wa Yesu Khristu" kudamupangitsa Yohane kutha kulemba buku la Chibvumbulutso (Chibvumbulutso 1:1-3) gulu lomaliza la anthu okhulupirira lidzalandiranso mphatso yomweyo: Maumboni ochokera kwa mwini wake Mulungu kudza mwachindunji kwa mtumiki wa dziko lapansi. Mphatso yawo ya ulosi idzatsimikizira pa za Chibvumbulutso cha Mulungu pa za cholinga chawo ndi mapeto awo.

Akhristu a masiku otsirizawa akudziwikanso monga "Iwo amene amvera Mulungu posunga Malamulo ake" Iwowatu sangoteteza kokha ukulu wa Malamulo Khumi a Mulungu ayi, komanso amamvera powasunga iwo. Chikondi cha Mulungu m'mitima yawo chimabweretsa chimwemwe cha kumvera (Aroma 5:5; 13:8-10).

Akhristu a masiku omalizawa amatsatira chitsanzo cha Yesu Khristu ndi mpingo woyambirira pakutsatira ndi kumvera Malamulo a Mulungu. Izi zimakwiyitsa chinjoka-mdierekezi. Ndipo akumema nkondo ndi "Otsala" a "mbewu" ya mkaziyo chifukwa ali ndi umboni wakuti chikondi cha Mulungu chimabala akuphunzira ake omvera. Monga umene Yesu adalamulirira kuti:

'Ngati mukonda ine, sungani Malamulo anga." - Yohane 14:15.

Miyoyo ya a Khristu a masiku omalizawa ikuonetsera kuti ndizotheka kumvera Mulungu ndi kumukonda ndi mtima wathu wonse, komanso kukonda nzathu monganso ife eni. Malinga ndi Yesu, zizindikiro izi,

chikondi pa Mulungu ndi pa anthu ena, zikumanga malamulo onse khumi pamodzi kupanga lamulo lalikuru (Mateyu 22:35-40).

Lamulo lachinayi la iwo likutifunsa kusunga Sabata, tsiku lachisanu ndi chiwiri la pa Mulungu. Ndipo popeza chikondi cha pa Mulungu chagonera pa kukhazikika kwa Malamulo onse Khumi a Mulungu m'mitima yawo, a Khristu a masiku a kumapeto kwa nthawiwa ndi osunga Sabata.


Sabata ndilo mtima wa uthenga wace wa Mulungu wotsiriza kwa anthu ake m'Chibvumbulutso, mitu ya khumi ndi chiwiri, ndi khumi ndi chinayi (14:6-15) zonse zofunikara za kumwamba zaonetseredwa mwa okhulupirira a masiku otsirizawa polongoseledwa mu mitu imeneyi; Mpulumutsi wa moyo ndi yemwe ali ndi iwo monga bwenzi, ndipo Mzimu Woyera akugwira ntchito "kuwalimbikitsa mu mphamvu za mka ti mwawo monga anthu". Lonjezo iri lokhazikika ndithu. Adzagonjetsa satana "ndi mwazi wa Mwana wa Nkhosa ndi mau a umboni wawo" (Chibvumbulutso 12:11).

Kodi inu mukufuna kukhala mmodzi wa a Khristu a mmasiku omaliza amene "omvera Malamulo a Mulungu" ndiponso "kukangamira pa umboni wa Yesu"? Bwanji kodi osapanga chitsimikizo choterechi tsopano lino?

KODI MULUNGU ALI NAWO UTHENGA WAPADERA WA NTHAWI YATHU INO

Ramoni Umashankar anabadwa mufuko la ansembe a chi Hindu la Bramini. Akali wamng'ono, akulu ake adamphunzitsa kuti iye anali mulungu, ndi kuti pofuna kuuzindikira umulungu wake iye anayenera kuchita utumiki wakudziletsa ndi kusinkhasinkha mwauzimu molingana ndi chipembedzo cha chi Hindu.

Ramoni anayamba kufufuza Baibulo ndi zomwe Khristu amanena. Iye nthawi zonse analemekeza Yesu chifukwa cha kuzichepetsa kwake, komano tsopano Ramoni anamva kuti Yesu ameneyu anazitchula yekha kuti analidi Mwana wa Mulungu. Iye anazindikira kuti Akhristu ambiri amaoneka kuti anali ndi mtendere umene zaka zambiri zakusinkhasinkha mwauzimu kunalephera kupereka. Komabe Ramoni anatsimikiza mtima kuti achipeze choonadi mu chipembedzo chake cha chi Hindu.



Koma kenaka iye anaonera kanema wa moyo wa Khristu. Kwa nthawi yoyamba iye anazindikira kuti Yesu nakumana nacho chizunzo ndi mantha monga munthu wina aliyense. M'mbuyomo iye ankaganiza kuti Yesu mwina anagwiritsa ntchito mphamvu yake ya umulungu kuti apulumuke ku kuwawa kwa kupachikidwa. Koma tsopano iye analephera kuufotokoza mtanda. Iye anadabwa; Zinatheka bwanji Yesu ameneyu kupyola chivuto ngati chimenechi - chifukwa chaanthu ochimwa?

Potsiriza kusinkhasinkha za imfa ya Khristu, Ramoni anakutidwa ndi chionetsero chotere cha chikondi. Iye anatsimikiza kusiya chi Bramini chosilirikacho ndi kupereka moyo wake kwa Yesu, Mpulumutsiyo. Poyerekeza ndi chikondi chodzipereka nsembe cha Yesu, Ramoni anati, "Zina zonse zinasanduka zopanda pake."

M'nyamata uyu wa chi Bramini anapeza chilikati chenicheni cha choonadi cha chikhristu: Yesu, Mpulumutsi wa dziko lonse lapansi.

1. NDI CHIPEMBEDZO CHITI CHOMWE CHIMAPULUMUTSA?

Yesu ndiye njira - njira yokhayo basi - ya chipulumutso.

"Ndipo palibe chipulumutso mwa wina yense, pakuti palibe dzina lina pansi pa thambo lakumwamba, lopatsidwa mwa anthu, limene tiyenera kupulumutsidwa nalo." - Machitidwe 4:12.

Baibulo limaphunzitsa momveka bwino kuti ife ndife otayika mu uchimo, ndi kuti motero taikika ku chilango cha uchimo: imfa (Aroma 6:23). Onse anachimwa (Aroma 3:23), chotero onse ayang'anana ndi imfa. Ndipo ndi Yesu yekha - iye yekha basi- amene angatipulumutse ife ku kutsutsidwa kwa uchimo.

"Yense wakuyang'ana mwana, ndi kukhulupirira iye, ali nawo moyo wosatha; ndipo Ine ndidzamuukitsa iye tsiku lomaliza." - Yohane 6:40.

Pali chipembedzo chimodzi chokha choona:

"Ambuye mmodzi, chikhulupirorilo chimodzi, ubatizo umodzi." - Aefeso 4:5.

2. KODI MULUNGU ALI NAWO UTHENGA WAPADERA KWA AKHRISTU A M'MASIKU OMALIZA?

Inde. Uthenga uwu wa mbali zitatu umapezeka mu Chibvumbylutso 14:6-16. Kulalikidwa kwa mauthengawa kolalikidwa ndi angelo awa atatu kukumalizira ndi kudza kwachiwiri kwa Khristu (mavesi 14-16).



(1) Uthenga wa Mngelo Woyamba

"Ndipo ndinaona mngelo wina alikuuluka pakati pa mlengalenga, wakukhala nawo Uthenga Wabwino wosatha, aulalikire kwa iwo akukhala pa dziko, ndi kwa mtundu uli wonse ndi pfuko ndi manenedwe ndi anthu; ndi kunena ndi mau akuru, Opani Mulungu, Mpatseni ulemerero. Pakuti yafika nthawi ya chiweruziro chake; ndipo mlambireni lye amene analenga m'mwamba ndi mtunda ndi nyanja ndi akasupe amadzi." - Chibvumbulutos 14:6, 7.

Ngakhale malembo Oyera akuonetsera mwachindunji mauthenga atatu awa kupiyolera mu phiphiritsa la angelo atatu, anthu a Mulungu ndiwo amene ali amithenga oulalikira uthenga ku dziko lonse lapansi - Iwotu sakulalikira uthenga wina watsopano , koma "Uthenga womwewo wosatha" ku dziko lonse lapansi - "Kwa mtundu uli wonse, ndi pfuko ndi manenedwe ndi anthu." Uthenga uwu wosatha" wa Yesu ndi uthenga womwewo wa chipulumutso womwe anthu a m'nthawi ya m'chipangano chakale anaulandira "mwa chikhulupiro" (Ahebri 3:16-19; 4:2; 11:1-40); chiphunzitso chomwecho chimene Yesu Mwini anachilalikira; uthenga womwewo akuphunzira (aphunzi) anaulalikira pomgonjetsa Yesu dziko lapansi; uthenga womwewo umene wagwedeza dzikoli mu zaka mazana-mazana a nyengo ya chikhristu.

Uthengawu, wofewa ndi wa chindunji, wopulumutsa wa Yesu Khristu, udatsala pang'ono kuzimira kuchoka mu mpingo kwa zaka zoposera zikwi mu nthawi ya mdima, koma nthawi yakukonzanzo inaubwezeranso, ndipo anthu a Mulungu akuulalikira ku dziko lonse lero. Mngelo woyambayu akulalikira uthenga wabwino womwewu, komanoakuupereka mu chikhazikitso chatsopano - chakuta dziko lonse lapansi - kwa anthu omwe akukhala mmasiku oyang'anana ndi kudza kwa chiwiri kwa Yesu.

Iwo amene akuulandira uthengawu akudzipeza okha akuitanidwira ku "kuopa Mulungu ndi kumpatsa ulemerero (kuonetsera khalidwe Lake)". Iwo akulionetsera dziko lonse khalidwe la Mulungu lachikondi, osati m'mau awo okha ai, komanso m'moyo wao wochitira umboni. Iwo akupereka chibvumbulutso chopatsa chidwi cha zomwe Mulungu angachite kudzera mwa anthu odzazidwa ndi Mzimu wa Khristu.



Kodi ndi nthawi iti imene mauthenga awa a angelo atatu ayenera kulalikidwa kudzikoloNSE lapansi? Ndi nthawi imene ola la "Chiweruziro cha Mulungu lafika." Phunziro 13 akufotokoza kuti Yesu anayamba ntchito ya chiweruziro chake chofufuza mu 1844. M'chaka chomwecho, 1844, Yesu anauzirira ndi Mzimu Wake anthu ambiri padzikoloNSE kudzera mu anthu kudzera mwa anthu odzazidwa ndi Mzimu wa Khristu.

Uthenga umenewu ukutiitana ife tonse kuti "timulambire lye amene analenga m'mwamba, (ndi) dziko" (Chibvumbulutso 14:7). Mulungu akutiitana ife tonse kuti "tizikumbukira tsiku la Sabata pakulisunga kuti likhale loyera" chifukwa "m'masiku asanu ndi limodzi Yehova adamaliza zakumwamba ndi zapansi (Eksodo 20:8-11). Mu chaka cha 1844 pamene Darwin anali kulenga ndi kuphunzitsa za chilengedwe kudzera mu kusintha sintha kwa zinthu, Mulungu naye anali kuitana anthu kuti azipembedza lye monga Mlengi wao ndi wa zinthu zonse. Pa nthawi yokhayokhayi, iwo amene anali kulalikira mauthenga awa a angelo atatu, anapeza Sabata la tsiku lachisanu ndi chiwiri la m'Mau a Mulungu nayamba kulisunga pakufuna kulemekeza Mlengi wa kumwamba ndi dziko lonse lapansi.

(2) Uthenga wa Mngelo Wachitatu

"Ndipo anatsata mngelo wina mnzake ndi kunene, Wagwa, wagwa Babulo waukulu umene unamwetsako mitundu yonse ku vinyo wa mkwiyo wa chigololo chake." - Chibvumbulutso 14:8.

Mngelo wachiwiriyu akuchenjeza "wagwa Babulo wamkulu" Chibvumbulotso 17 amaonetsera "Babulo" wauzimu - chikhristu chachipatuko - monga ngati mkazi wachigololo (vesi 5). Iye waima motsutsana ndi mkazi woyera wa m' Chibvumbulutso 12 amene akuimira mpingo woona wa chikhristu. Mkazi uyu yemwe akuimira Babulo ndi mkazi wakugwa yemwe "anamwetsako mitundu yonse ku vinyo wa mkwiyo wa chigololo chake" Vinyo wa chipunxitso chonyenga walowerera mu ziphunxitso zonyenga zonse za chikhristu. Uthenga uwu wa mngelo wa chiwiri ukuitana anthu onse a Mulungu kuti akane ziphunxitso zonyengazi za chikhristu cha mpatukochi.



Babulo akuimira chisakanizo cha mitundu yambiri ya chikhristu champatuko. Iyeyu ndi woopsyka kwambiri chifukwa amasokoneza ndi kukwiwaykiya chithunzi cha Mulungu ndipo chimaoneka ngati chipukwani chamafupa okhaokha: Mulungu motero amaoneka ngati wa nkhanza ndi wobwezera, kapena ngati gogo wokoma mtima molekerera kwambiri mwakuti sasamala ngakhale wina azichita uchimo. Mpingo woona ndi wanthanzi la umulungu udzaonetsera chithunzi cheni cheni cha makhalidwe onse a Mulungu pamodzai ndikuonetseranso mmene chilungamo chake ndi chifundo zimagwirizirana ndi choonadi chakuti Mulungu ndiye chikondi.

Mulungu akuitana anthu kuti "atuluke mu Babulo" (Chibvumbulutso 18:4), pokana ziphunxitso zosachokera mu Baibulo ndi kutsata ziphunxitso za Khristu Yesu.

(3) Uthenga wa Mngelo Wachitatu

"Ndipo anawatsata mngelo wina, wachitatu, nanena ndi mau akulu, 'ngati wina alambira chilombocho, ndi fano lake, nalandira lemba pa mphumi pake, kapena padzanja lake, iyenso adzamwako ku vinyo wa mkwiyo wa Mulungu, wokonzeka wosasanganiza m'chikho cha mkwiyo wake; ndipo adzazunzika ndi moto ndi sulfure pamaso pa angelo oyera mtima ndi pamaso pa Mwanawankhosa, ndipo utsi wa kuzunza kwao ukwera ku nthawi, ndipo sapuma usana ndi usiku iwo akulambira chirombocho ndi fano lake, ndi iye ali yense akalandira lemba la dzina lake. Pano pali chipiliro cha oyera mtima, cha iwo akusunga malamulo a Mulungu, ndi chikhulupiriro cha Yesu." - Chibvumbulutso 14:9-12.

Uthenga wa mngelo wachitatuwu ukugawa dziko lonse m'magulu awiri. Ku mbali imodzi kuli Akristu a mpatuko omwe "amalambira chirombo ndi fano lake ndi kulandira lemba lake pamphumi kapena pa dxanja lawo." Ku mbali inayi kuli iwo amene amakana ulamuliro wa chirombo, "Oyera mtima" amene "amamvera malamulo a Mulungu ndi kukhala okhulupirika kwa Yesu."

Taonani kusiyana kumene kulipo pakati pa magulu awiri otsutsanawa. Iwo amene alandira lemba la chirombo ndi opembedza amene amagwetsa pansi mbendera za chi Khristu choona natsata ziphunxitso ndi nzeru za anthu zimene zimawakomera. "Oyera mtimawa" ali ndi chikhaldwe chowasiyanitsa ndi opandukawa. "Kupirira" kumvera malamulo a Mulungu, ndi "Kukhalabe okhulupirika kwa Yesu".

Mauthenga atatu ogwirizanawa atalalikidwa ku dziko lonse la pansi, Yesu adzabwera "Kudzakolola" opulumutsidwa.

"Ndipo ndinapenya, taonani, mtambo woyer'a ndi pamtambo padzakhala wina monga Mwana wa munthu, wakukhala naye korona wa golidi pamutu pake, ndi m'dzanja lake zenga



Iakutwa. Ndipo mngelo wina anatuluka m'kachisi, wopfuula ndi mau akulu kwa lye wakukhala pa mtambo. 'Tumiza zenga lako ndi kumweta, pakuti yafika nthawi yakumweta; popeza dzinthu dza dziko dzachetsa'. Ndipo iye wokhala pamtambo anaponya zenga lake padziko, ndipo dzinthu dza dziko dzinamwetedwa." - Chibvumbulutso 14:14-16.

3. MPINGO WA KHRISTU WA MMASIKU WOTSIRIZA

Kodi mudayamba mwamyamikira Mkhristu wamphamvu, wokhazikika, m'mudabwa kudzipereka, chipiriro ndi chikhulupiro zoceanali nazo ndi kulakalaka kukhala nawo machitidwe auzimu monga akewo? Mulungu anaperekwa uthenga Wake wapadera wa m'masiku athu ano mu Chibvumbulutso 14 chifukwa iwo ungtututse machitidwe a chikhaliidwe ngati cha mkhristu ameneyu.

Monga kudafotokozedwa mu Phunziro 25, Chibvumbulutso 12:17 amazindikiritsa Akhristu am'masiku omaliza monga "iwo amene asunga malamulo a Mulungu, nakhala nawo umboni wa Yesu." Chibvumbulutso 14:12 akulifotozo gulu lomweli monga "Oyera mtima amene asunga malamulo a Mulungu, ndi chikhulupiro cha Yesu."

Tatiyeni timange pamodzi mwachidule makhalidwe awa a Akhristu a m'masiku omaliza.

(1) Iwo "ali nawo umboni wa Yesu"

Ngakhale pamene Satana awatulutsira ukali pa iwo, iwo "amakhalabe wokhulupirika kwa Yesu. "Chikhulupiro chawo sichongodzipangira mwa iwo wokha ai, chili mphatso yochokera kwa Mulungu (Aefeso 2:8). Mpingo wa Mulungu wa m'masiku otsiriza udzimuona Yesu Khristu moonekera koposa mu chikhaliidwe chake choona ndipo mwachisomo chodzera mu chikhulupiro Akhristu ake a mpingowu azikhala monga zipilala za moyo zoonetsera mphamvu ya Khristu yokha mkatı mwao.

(2) Iwo "asunga ... chikhulupiro cha Yesu" (Chibvumbulutso 14:12). Chikhulupiro chimene Yesu anali nacho, chimene lye adaphuzitsa, chikhulupiro chimene lye anachikhala m'moyo Wake, tsopano chidzaza m'mitima yawo. Iwo samangokhala nacho choonadi choka ai, "amasunganso" choonadi - amachitsatira. Kwa iwo chipembedzo ndiye moyo, chikhulupiro chilamulira chikhaliidwe ndi zochita zawo, ndipo chiphatikizana ndi kumvera. M'moyo wao watsiku ndi tsiku "chikhulupiro cha Yesu" chionekera. Iwo apeza kuti ziphunzitso zazikulu za m'Baibulo zikagwiritsidwa ntchito m'myoyo wa tsiku ndi tsiku, zimatulutsa moyo wochitachita wa chikhristu. Iwo apeza kuti zoonadi zikuluzikulu za m'baibulo zimadzutsa chikondi ndi kudzipereke kwa Khristu komwe kumakwanitsa chosowa chilichonse ndi cholakalaka chilichonse cha mtima wake wa munthu.

(3) Iwo amasunga (amamvera) malamulo a Mulungu" -
malamulo khumi, lamulo la chikhaliidwe la Mulungu.

Koposa zonse iwo amafuna kumvera chifuniro chilichonse cha Mulungu, ndi lamulo lake lililonse. Iwo amasonetsa chikondi chawo kwa Mulungu ndi kwa anthu ena onse pakutsatira malamulo onse a Mulungu, kuphatikizapo lamulo lachinayi limene limatilangiza kupembedza Mlengi wathu pa kuyeretsa Loweruka, lomwe lili Sabata la tsiku lachisanu ndi chiwiri.

(4) Iwo amagawira ena "uthenga wabwino wosathawu" ku dziko lonse lapansi (Chibvumbulutso 14:6).

Uthengawu umanenetsa kuti Yesu adafera machimo athu, kenaka nkuuka kwa akufa kuti ife tikhale nawo machitidwe a chiyanjano cha chipulumutso ndi lye. Mpingo wa Khristu wa m'masiku otsiriza wakhala ukitanira anthu kulikonse kuti atuluke mu chisokonekero cha chipembedzo ndi kulumikizana ndi Yesu potsatira choonadi cha m'Baibulo mokha basi.



(5) Iwo amakhala ndi **chikakamizo cha changu m'moyo wao** chifukwa "yafika nthawi yakumweta; popeza dzinthu dza dziko adzachetsa" (Chibvumbulutso 14:15), ndipo miyanda miyanda ya anthu siinampezebe Khristu.

(6) **Iwo atengeka ndi utumiki wopatsidwa ndi Mulungu.** Chifukwa "Babulo wamkulu" akugwa, iwo akudandaulira anthu awo amene akukhalabe mu chipembedzo chosokonekeracho, "Tulukani m'menemo, anthu anga" (Chibvumbulutso 18:4). Iwo akufuna kugawana ndi aliyense chiyanjano chodabwitsa ndi chawo zimene ali zimene ali nazo mwa Khristu.

Izi zonse ndi zina zambiri zimalunzanitsa pamodzi mitima ya miyanda miyanda ya Akhristu a m'masiku otsiriza omwe adaitanidwa ndi mauthenga a angelo atatuwa. Moyo walo wachimwemwe umawatsogolera iwo kulumikizana ndi mtundu Yohane pakukuitanani uku:

"Tikulalikirani inunso, kuti inunso mukayanjane pamodzi ndi ife; ndipo chiyanjano chathu chilinso ndi Atate, ndipo ndi Mwana wake Yesu Khristu; ndipo izi tilemba ife, kuti chimwemwe chathu chikwaniridwe." - 1 Yohane 1:3, 4.

Kudzera mwa Mzimu Wake ndi mwa mpingo Wake, Yesu akukuitanani inunso kuti mudze ndi kupereka zonse kwa lye.

"Ndipo Mzimu ndi mkwatibwi anena, Idzani: Ndipo wakumva anene, 'Idzani' Ndipo wakumva ludzu adze; iye wofuna, atenge madzi a moyo kwaulere." - Chibvumbulutso 22:17.

4. MAKHOLOLA AWIRI

Mauthenga awa a angelo atatu afika kumapeto kwake pamene Yesu adzanso ku dziko lino kudzakolola opulumutsa a mibadwo yonse (Chibvumbulutso 14:14-16). Yesu asonhanitsa opulumutsidwa onse nawatengera iwo ku "Malo okhalamo ambiri" Kumwamba (Yohane 14:1-3). Lye tsopano achotsa kwa nthawi zonse uchimo, matenda, zisoni ndi imfa. Oyera mtima tsopano ayamba kukhala miyoyo yaho yatsopano ndi lye zaka zamuyaya (Chibvumbulutso 21:1-4).



Yesu "adzakololando" oipa pakudza Kwake:

"Ndipo mngelo wina anatuluka m'Kachisi ali m'Mwamba, nakhala nalo zenga lakuthwa nayenso. Ndipo mngelo wina anatuluka pa guwa lansembe, ndiye wakukhala nawo ulamuliro pamoto; nafuula ndi mau akulu kwa iye wakukhala nalo zenga lakuthwa, nanena, Tumiza zenga lako lakuthwa, nudule matsango a munda wampesa wa m'dziko; pakuti mphesa zake zapsa ndithu. Ndipo mngelo anaponya zenga lake ku dziko, nadula mphesa za m'munda wa m'dziko, naziponya moponderamo mphesa mwamukulu mwa mkiyo wa Mulungu. Ndipo moponderamo mphesa anamuponda kunja kwa mzinda, ndipo mudatuluka mwazi moponderamo mphesa." - Chibvumbulutso 14:17-20.

Iyitu idzakhala nthawi yoopsy ya chionongeko chotsiriza chochitika chomvetsa chisoni kwa Khristu chifukwa lye ayenera kuwaononga awo amene anakana kupulumutsidwa. Yesu "aleza mtima kwa inu, wosafuna kuti ena aonongeke, koma kuti onse afike kukulapa" (Petro 3:9).

Pamene Yesu akubwera kudzakolola khola la dziko, kodi inu mudzakhala mu kholola liti? Kodi mudzaima pakati pa tirigu wakucha pamodzi ndi oomboledwa a mibadwo yonse (Chibvumbulutso 14:13-16)? Kapena mudzakhala pakati pa mphesa zakucha zachionongeko pamodzi ndi otaika (mavesi 17-20)?



Nkhaniyitu yafotokozedwa momveka bwino. Ku mbali imodzi, Yesu waima atatambasula manja ake okhomedwa misomali, kukudandaulirani inu kuti mutenge mbali yanu pamodzi ndi "oyera mtima amene" asunga malamulo a Mulungu, ndi chikhulupiro cha Yesu (vesi 12). Ku mbali inayi ku mau a anthu wamba, amene akunena motsindika kuti kumvera zonse za m'Baibulo ndi malamulo onse a Mulungu sizofuni ka kweni-kweni ai.

Chikhamu cha anthu m'bwalo loweruzira milandu la Pilato lidakhalanso ndi machitidwe okhaokhawa. Ku mbali imodzi kunali Yesu, Mulungu-munthu, Ku mbali inayi kunali Baraba, munthu

wosowa chithandizo, yemwe sakadatha ngakhale kudzithandiza yekha kapena iwo a mu chikhamuchi amene ankachitira umboni zonsezi. Komabe pamene mau a ulamuliro a Pilato anamvekera poneponse, "Ndi ndani wa awiri amene ndikumasulireni?" chimkokomo ca anthu wokwiya chidayankha, "Baraba"

"Nangano" adafunsa Pilato, "ndidzachita naye chiyani Yesu, wotchedwa Khristu?"

Mogwirizana, chikhamucho chidafuula, "Apachikidwe pa mtanda!" Motero Yesu, Wosachimwayo, adapachikidwa pa mtanda; ndipo Baraba, wopalamulayo, anamasulidwa (Onani Mateyu 27:20-26).

Nanga inu musankha yani lero, Baraba kapena Yesu? Kodi musankha kutsatira maganizo opangidwa ndi anthu ndi ziphunzitso zomwe zili zothutsana ndi malamulo a Mulungu ndi uthenga wosatha wa Yesu? Kapena mufuna "kumvera malamulo a Mulungu ndi kukhala okhulupirika kwa Yesu"? Kumbukirani, Yesu ndiye amene alonjeza kutumiza Mzimu Wake Woyeru kuti akuthangateni mu chivuto chanu chili chonse, achize kusweka mtima kwanu, ndi kukwanitsa chokhumba chanu chilichonse.